

Nkhondo Ya Thupi

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

© Harvestime International

Institute <http://www.harvestime.org>

ZAMKATI MWA BUKULI

Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu	4
Chiyambi	5
Zolinga Za Phunziroli	8

GAWO LOYAMBA:

NKHONDO YA THUPI

1. Nkhondo Ya Maufumu	10
2. Kuyitana Ku Zida Za Nkhondo	20
3. Nkhondo Isanayambe	26

GAWO LACHIWIRI:

CHIWEMBU

4. Gwero La Matenda	34
5. Zifukwa Za Matenda	40
6. Mitundu Ya Matenda	47
7. Zotsatira Za Matenda	52

GAWO LACHITATU:

KUBWEZERA CHIWEMBU

8. Maziko Amachiritso a M'baibulo	57
9. Zolinga Za Machiritso	83
10. Mphatso Za Machiritso	89

GAWO LACHINAYI:

KUGONJETSZA ZONTCHINGA

11. Chikhalidwe Cha Anthu	97
12. Minga M'thupi	108
13. Mafunso Opanda Mayankho	114

GAWO LACHISANU:

NDONDOMEKO ZAMACHIRITSO

14. Mmene Mungatumikire Ndi Kulandira Machiritso	130
15. Utumiki Olondola Onse Amene Achiritsidwa	139
16. Machiritso Amtheradi	147

GAWO LACHISANU CHIMODZI:

NDONDOMEKO ZA MAMASULIDWE

17. Kodi Ndindani Amene Satana Wamumanga.	155
18. Kutumikira Mamasulidwe	170
19. Utumiki Wolondola Wamamasulidwe	181

GAWO LACHISANU NDI CHIWIRI:

CHIKHALIDWE CHA UFUMU WA MULUNGU

20. Omenya Nkhondo Abwino	187
Pomaliza	196
Zakumapeto A: Kusathula Mwakauniuni	198
Zakumapeto B: Maziko A M'baibulo a Machiritso Ndi Mamasulidwe	204
Zakumapeto C: Fomu Ya Kauniuni	220
Mayankho a Mafunso Oziyesa Nokha	221

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Nchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunzeni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

PHUNZIRO: NKHONDO YA THUPI

CHIYAMBI

Mpingo woyomba umatenga zokamana nazo ngati nkhondo. Mawu okamba nkhondo agwiritsidwa mu Chipangano Chatsopano chonse. Chitetedzo chinaonedwa ngati zida za nkhondo za Mulungu. Mawu a Mulungu anafananidzidwa ndi lupanga. Ziwembu cha Satana zinatchedwa kuti mibvi. Chikhuupiriro chinali “kumenyana kwabwino” ndi okhulupirira anaudzidwa “kumenya nkhondo yabwino.” Mpingo woyamba unadzindikira kuti unali pa nkhondo yayikulu.

Baibulo limanena kuti anthu a Mulungu akuonongeka chifukwa chakutsadziwa (Hoseya 4:6). Mbali imodzi imene okhulupirira amagonjetsedwa chifukwa cha kutsadziwa ndi mbali ya nkhondo yosaoneka. Pali nkhondo yayikulu imene ikumenenya pa dziko lero. Si nkangano wapakati pa mayiko, mitundu, kapena adzitsogoleri a ndale. Ndi nkhondo yofunikira ya mu dziko la uzimu.

Moyo ya Chikhristu ndi nkhondo. Tikadzindikira nsanga ndi kukonzekera, tikhala opambana. Mbali imodzi ya nkhondo yosaonekayi imalunjikira ku moyo ndi mzimu wa munthu. Phunziro la Harvestine International Institute ya “*Ukadaulo wa Uzimu: Mlozo wa Nkhondo ya Uzimu*” omwe ukukamba za nkhondo ya uzimu yosaoneka.

Koma palinso mbali yina ya nkhondo yomwe imaonetseredwa mu dziko la kuthupi. Mu phunziroli talitchula “*Nkhondo la Thupi.*” Satana akulimbana ndi matupi a okhulupirira chifukwa akudziwa kuti matupi a anthu ankhondo ofooka ndi odwaladwala sangalimbane nkhondo yopindula kulimbana ndi ufumu wake.

Luka 14:31 akuti “Kapena mfumu yanji pakupita kukomana ndi nkhondo ya mfumu inzace, sathanga wakhala pansu, nafunsana ndi akuru ngati akhoza ndi asilikari ace zikwi khumi kulimbana naye wina uja alikudza kukomana naye ndi asilikari zikwi makumi awiri?” Ayi palibe amene akuyenera kulowa mu nkhondo asanafufuze bwinobwino za zida zake ndi momwe angakamenyere nkhondo.

Mu phunziro iri tikuona mtsamala za njira zomwe ziripo kuti tikakhale wopambana pa nkhondo yolimbana ndi Satana pa nkhoti ya thupi lanu. Muphunzira kumenya nkhondo ya khupi lanu ndi kutumikira choonadi ichi kwa atsirikali ena omwe abvulala a Mulungu.

BUKULI

Bukulo lagawidwa mu magawo asanu ndi awiri:

GAWO LOYAMBA: Nkhondo ya Thupi ikukamba nkhondo yosaoneka pakati pa Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Satana. Mulonso kuyitana anthu ku zida za nkhondo ndi kupereka kakonzekeredwe ka nkhono koyambirira.

GAWO LACHIWIRI: Chiwembu chikukamba gwero, zifukwa, mittundu, ndi zotsatira za matenda

GAWO LACHITATU: Kubwezera chiwembu ikupereka njira zogonjetsera mdani pamene mukupedza kumvetsetsa maziko a machiritso a m’Baibulo, zolinga za machiritso, ndi mphatso za machiritso.

GAWO LACHINAYI: Kugonjetsa zontchinga ikumamba zotchinga za utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe kuphatikidzira zikhaliidwe za anthu, minga mu thupi la Paulo, ndi mayankho osayankhidwa.

GAWO LACHISANU: Ndongomeko zamachiritso imakupatsana njira zotumikira machiritso, utumiki wamachiritso oyendera anthu, ndi machiritso okhazikika.

GAWO LACHISANU CHIMODZI: Ndongomeko za mamasulidwe ikukamba za utumiki wamamasulidwe mu maphunziro oti “Amene Satana wamumanga,” “Kutumikira mamasulidwe,” “Utumiki wa mamasulidwe woyendera anthu.”

GAWO LACHISANU NDI CHIWIRI: Chikhalidwe cha ufumu wa mulungu ikukamba njira za chitetezo ndi zothandiza zochokera Mawu a Mulungu zomwe zingakupangitseni kukhala nsilikari wabwino, yemwe ali wangwiro ku thupi, moyo ndi uzimu okonzekera kukamenya nkhondo

MATHERO a bukuli akupereka zophunira zina za m’Baibulo zowonjezera pa utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe. Komanso muli kusanthula kwa kauniuni komwe kangakuthandizeni kufuna komanso kutumikira machiritso.

MAPHUNZIRO

Phunziro ina iliyonse yakonzedwa motere:

ZOLINGA: Izi ndi zolinga zomwe mukuyenera kukwaniritsa pophunzira phunziro.

LONJEZO LA MACHIRITSO: Iyi ndi lonjezo lamachiritso lapaderadera lochokera mu Mawu a Mulungu kwa inu lomwe mukuyenera kulitenga pa moyo wanu.

CHIYAMBI: Chiyambi chikupereka mwachidule zomwe ziri mkati mwa chaputala.

PHUNZIRO: Gawo iri likukamba malangizo a momwe mungamenyere nkhondo.

MAYESO OZIYESA NOKHA: Mayeso oziyisa nokha amafunsa pa zinthu zomwe mwaphunzira.

KUCHITA MAWU: Baibulo limati “gwirani nchito yace ya cipulumutso canu ndi mantha, ndi kunthunthumira” (Afilipo 2:12). Pomwe mungaphunzire mu phunzirori, machiritso ali mbali imodzi ya chipulumutso chimene chinaperekedwa kudzera mu imfa ndi kuuka kwa Yesu Khristu. Chikhulupiriro ndi ntchito zimagwira tchito limodzi. Chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa, monga ntchito zopanda chikhulupiriro ndichopanda pake (monga ntchito zopanda chikhulupiriro ndichopanda pake (Yakobo 2:17-26).

Mu gawo lotchedwa “Kuchita mawu,” inu mutenga lingaliro lomwe mwaphunzira ndi kuligwiritsa ntchito moyo mwanu. Iyi ndi gawo lofunikira la phunziro. Ngati mukudwala, lakonzedwa kuti kuti likuthandizeni kulandira machiritso ano. Ngati mukutumikira kwa munthu yemwe akudwala, choyamba akagawireni zomwe zalembedwa mu phunzirori kenako malizani “Kuchita mawu” limodzi kuti muwathandize kuti alandire machiritso.

KODI MWAKONZEKA?

Kuyika pa mbalambanda mdaniyo ndi njira zake ndi limodzi mwa mabvumbulutso a Mau a Mulungu. Buku ili si buku lotopesa, koma ndilokamba mwadongosolo zinsinsi za Uzimu.

ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kuonetsera kumvetsetsa kwa dziko la kuthupi ndi lauzimu.
- Kutanthauza “nkhondo ya uzimu.”
- Kudzindikira chifukwa cha nkhondo yosaoneka.
- Kukamba mfundo zomvetsetsera nkhondo ya uzimu.
- Kutanthauza “machiritso aumungu”
- Kutsiyanyitsa pakati pa machiritso ndi mamasulidwe.
- Kufotokoza mene machiritso ndi mamasulidwe amakhuzanirana ndi ntchito yokafikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino.
- Kudzindikira gwero la matenda.
- Kufotoka zifukwa za matenda.
- Kudzindikira mitundu ya matenda.
- Kulemba zotsatira za matenda.
- Kulemba mwachidule maziko a machiritso a m’Baibulo.
- Kulemba zolinga za machiritso.
- Kumvetsetsa ndi kugwiritsa ntchito mpatso za machiritso.
- Kuyankha ku zikhaliwe za anthu zokhuzana ndi machiritso.
- Uthana ndi mafunso omwe sanayankhidwe okhuzana ndi machiritso.
- Kutumikira ndi kulandira machiritso.
- Kutumikira ndi kulandira mamasulidwe.
- Kuwakonzekeeretsa anthu ku machiritso okhazikika.
- Kupanda utumiki woyendera athu wamachiritso ndi mamasulidwe.
- Kulemba mwachidule malangizo akukhala moyo wa usilikari.
- Kumenya nkhondo wopindula pa nkhondo ya thupi.

GAWO LOYAMBA

NKHONDO YA THUPI

Pali nkhondo yayikulu yomwe ikumenyedwa mu dziko lauzimu. Ndi nkhondo yolimbana pakati pa thupi ndi mzimu, ndi nkhondo yolimbana ndi mphamvu zakumidima. Ndi nkhondo ya uzimu yolimbana ndi mphamvu zoipa za uzimu. ndinkhondonso yakuthupi, yomwe imalimbana ndi matupi athu omwe ali kachisi wa Mzimu Woyera.

Mu Chipangano Chakale lipenga limagwiritsidza ntchito pofuna kuyitanira anthu a Mulungu ku nkhondo. Lero, kuitana kwa uzimu kukuchitika pa dziko lonse lapansi. Ndi kuitana ku nkhondo yosaoneka. Ndikuitana ku zida za nkhondo.

CHAPUTALA 1

NKHONDO YA MAUFUMU

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kuonetsera kumvetsetsa kwa maufumu a kuthupi ndi uzimu.
- Kutanthauzira mawu ofi “mfumu.”
- Kutanthauzira mawu oti “ufumu.”
- Kudzindikira maufumu awiri auzimu.
- Kudziwa kuti ndinu a ufumu uti.
- Kudzindikira mphamvu zabwino za uzimu
- Kudzindikira mphamvu zoipa za uzimu.
- Kufotokoza tanthauzo la “nkhondo ya uzimu.”
- Kudzindikira chifukwa cha nkhondo yotsaoneka.
- Kufotokoza mfundo zofunikira zomvetsetsera nkhondo ya uzimu.

LONJEZO LA MACHIRITSO

...Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoonza pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)

CHIYAMBI

Pali nkhondo yayikulu yomwe ikuchitika pa dziko matsiku ano. Sinkhondo yapakati pa mayiko, mitundu, kapena adzitsogoreli a boma. Sizopandukira kapena zokhumba. Ndi nkhondo yotsaoneka yomwe ikuchitika mu dziko la uzimu. chaputala ichi chikuyamba kuonetsera nkhondo yotsaoneka yomwe okhulupirira aliyense akumenyana nawo. Ndi nkhondo yomwe palibe yemwe amavala yunifolomu, koma aliyense ndi amamenya nawo. Chiyambi cha nkhonkho imeneyi ndi mmene yakhala ikumenyedwera zalembedwa mu Mawu a Mulungu, Baibulo.

DZIKO LA THUPI NDI LA UZIMU

Kuti mumvetsetse nkhondo yosaoneka, mukuyenera kumvetsetsa kaye dziko la thupi ndi la uzimu. Munthu amakhala mu maiko awiri. Dziko la thupi ndi la uzimu. Dziko la thupi ndi dziko lomwe limaoneka, kukhuzidwa, kumveka, kapena kulawidwa. Ndilokhuzika ndi loonedwa.

Mayiko, mitundu, mizinda kapena midzi yomwe mumakhalamo iri m’mbali ya dziko lapthupi. Inu ndinu ikhala mu ufumu wa thupi lopezeka pa zilumba za dziko lapansi. Munthu kuona anthu

amene ali mbali imodzi ya chilengedwe. Mutha kulankhulana nawo. Mutha kukhuza, kumva ndi kuona zomwe zazungulira inu.

Komanso pali dziko lina lomwe inu mumakhalamo. Dziko la uzimu. simungathe kuliona ndi maso anu akuthupi, koma ndiloona ngati dziko laku thupi lomwe inu mumakhalamo. Pa 1 Akolinto 15:40, Paulo akaukamba za kusiyantsidwa kwa dziko la thupi ndi la uzimu. Akuti pali thupi la padziko ndi thupi la uzimu.

Anthu onse ali ndi thupi la pa dziko lomwe limakhala mu dziko la thupi, komanso munthu ndi munthu wa uzimu okhala ndi moyo ndi mzimu. Munthu ndi thupi, moyo ndi mzimu. Munthu wanu wa uzimu (moyo ndi mzimu) ali mbali ya dziko la uzimu momnga ngati thupi lanu la nyama ili mbali ya dziko la thupi.

KUYESA MU UZIMU

Chifukwa nthundo ya uzimu ndi ya uzimu, ikuyenera kumvetsetsedwa ndi malingaliro auzimu. Mumakhalidwe athu a thupi,

Koma munthu wa cibadwidwe ca umunthu salandira za Mzimu wa Mulungu: pakuti aziyesa zopusa; ndipo sakhoza kuzizindikira, cifukwa ziyesedwa mwauzimu. (1 Akorinto 2:14)

Nsizofunika kugwiritsa ntchito kuyesa kwa uzimu kuti tikamvetsetse zinthu za uzimu.

Mwina chitsanzo chimodzi chabwino cha kuyesa kwa thupi ndi uzimu chalembedwa pa II Mafumu mutu 6. Ndi nkhani ya nkhoona ya kuthupi yomwe ankhondo aku Siliya anazungurira dera laling'ono lotchedwa Dotani komwe Elisa anali kukhalako.

Pamene kapolo wa Elisa, Gehazi, anaona ankhondo a adani anayamba kuchita mantha. Elisa anapemphera kuti Mulungu atsegule maso auzimu a Gehazi kuti aone angelo ankhondoomwe awazungulira ndikuwateteza. Pa nthawi iyi, Mulungu anatseguladi maso akuthupi a Gehazi namulola kuti aone ankhondo a mphamvu a Mulungu omwe awazungurira iwo.

Nkhani iyi ya nkhoona ku Dotina imafanana ndi mmene zinthu za uzimu ziriri mu Mpingo matsiku ano. Pali ena, ngati Elisa, omwe amaona bwinobwino mu dziko la uzimu. amaziwa kuti pali nkhoona yomwe ikuchitika, adzindikira m'dani, ndikudzindikira mphamvu yayikulu ya Mulungu yomwe imatsimikiza chipambano.

Koma palinso ena ngati Gehazi, pakuwalimbikitsa mtima, akakwanitsa kutsegula maso awo auzimu ndi kutsiya kukhala a mantha. Mwachisoni, alipo anthu ambiri omwe, ngati iwo a mu mzinda wa Dotina, akungona mu uzimu. sakuzindikira kuti mdani wawazungurira ndipo akufuna amenyane nawo nkhoona.

MAUFUMU AWIRI A UZIMU

Mkati mwa mayiko a ku thupi ndi uzimu omwe tikukamba muli maufumu awiri omwe amalambuliridwa ndi azitsogoleri a ku thupi ndi uzimu.

UFUMU WAKUTHUPI:

Anthu onse amakhala mu ufumu wakuthupi wa dziko lino. Amakhala mu mdera kapena mudzi omwe uli mbali ya mtundu. Mtundu ndi ufumu wa dziko lino. Ufumu wa thupi ndi anthu omwe mfumu kapena mtsogoleri wan dale amakhala olamurira. Baibulo limakamba za maufumu athupi ngati “maufumu a dziko lapansi.” Maufumu a dziko lapansi ali pansu pa ulamuliro wa Satana:

Pomwense mdierekezi anamuka naye ku phiri lalitari, namuonetsa maiko onse a dziko lapansi, ndi ulemerero wao.

Nati kwa Iye, Zonse ndikupatsani Inu, ngati mudzagwa pansu ndi kundigwadira ine. (Mateyu 4:8-9)

Yohane 5:19 machisoni amatikumbutsa ife kuti “dziko lonse lapansi liri pansu pa ulamuliro wa Satana.”

MAUFUMU AUZIMU:

Pakuonjezera pa maufumu athupi palonso maufumu ena awiri a uzimu. Ufumu wa Satana ndi Ufumu wa Mulungu. Munthu wina aliyense wamoyo ndiwokhala mwa umodzi wa maufumuwa.

Ufumu wa Satana muli Satana, zamoyo za uzimu zotchedwa ziwanda, ndi anthu onse omwe amakhala mu tchimo ndi okana Mawu a Mulungu.

Ufumu wa Mulungu muli Mulungu Atate, Yesu khristu, Mzimu Woyera, zamomo zauzimu zotchedwa angelo, anthu onwe omwe amakhala moyo wachiyo omvera Mawu a Mulungu.

Ufumu wa Mulungu sichipembedzo. Zipembedzo ndi mabungwe opangidwa ndi anthu a magulu a mipingo. Zipembedzo ndi mabungwe a mipingo ikuluikulu ngati Baptist, Assembly of God, Methodist, Lutheran, ndi ena ambiri. Baibulo limakamba za Mpingo woona omwe suli wa chipembedzo kapena bungwe lachipembedzo. Mpingo umapangidwa ndi anthu onse omwe ali okhala mu Ufumu wa Mulungu.

Ufumu wa Mulungu umakhala mwa muhtu aliyense amene wapanga Yesu kukhala Mfumu ya miyoyo yawo. Imakhala limodzi mu mpingo woona and kulikonse komwe anthu omwe apanga dziko lapansi monga mmene Mulungu akufunira kuti likhale. Patsogolo, pazakhala kuonetseredwa kuona kwa ufumu wa Mulungu.

NKHONDO YOSAONEKA

Nkhondo ya uzimu yosaoneka ikukhuza anthu onse. Chifukwa Ufumu wa Satana ndi ufumu wauzimu...

...kulimbana kwathu sitilimbana nao mwazi ndi thupi, komatu nao maukulu, ndi maulamuliro, ndi akucita zolimbika a dziko lapansi a mdima uno, ndi a uzimu a coipa m'zakumwamba. (Aefeso 6:12)

Nkhondo ya uzimu si nkhondo ya kuphupi yapakati pa mwazi ndi thupi. Si nkhondo ya munthu ndi munthu. Ndi khondo ya uzimu. Ndi nkhondo ya mkati ndi kunjira kwa munthu. Si nkhondo yooneka chifukwa mizimu nayo ikukhuzidwa ndipo timaphunzira pa Luka 24:39 kuti mzimu ulibe mnofu ndi mafupa.

Nkhondo ya uzimu ndi:

1. Nkhondo pakati pa okhulupirira ndi dziko lapansi: Yohane 15:18-27
2. Nkhondo ya thupi ndi mzimu: Agalatiya 5:16-26
3. Nkhondo ya uzimu yapakati pa okhulupirira ndi mphamvu zakumidima: Aefeso 6:10-27
4. Nkhondo yakuthupi, yomwe satana amalimbana ndi matupi anu pakuyambisa matenda osiyanasiyana: Yobu 1-2

Munthu wina ali yense wamoyo ali pa nkhondo, kaya kuziwa kapena ayi. Palibe yemwe sakulipamba pa nkhondo. Osakhulupirira ali mu linga la oyipa ndipo atengedwa ukapolo ndi mphamvu ya m'dani. Iwo ndiwozuzidwa chifukwa cha nkhondo. Okhulupirira ali omatsulidwa kudzera mwa Yesu Khristu ndipo ndi agonjetsi, koma akadali kumenya nkhondo ngati asilikali.

Aefeso 6:12 imaonetsa kuti ife (okhulupirira) sitilimbana ndi maulamuriro a choipa. Palibe yemwe watsiyidwa ku nkhondo. Palibe yemwe amangoyang'anira patali. Inu muli nkatinkati mwa nkhondo kaya mukudzindikira kaya ayi. Ngati mumakhulupirira kuti muzasiya kumenyana, mukunama. Nkhondo ya a Kristu siyitha.

KOMWE NKHONDO IMACHITIKIRA

Nkhondo yosaonekayi ikuchitikira pa dziko lapansi:

Siikudza (pa dziko) mbala (Satana), koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Satana amamenya nkhondo ndicolinga choti adzilamulirabe dziko lapansi. Samufuna kuti iwo afike pansu pa ulamuliro wa Mulungu. Komanso nkhondoyi imachitikira mmitima, mmalingaliro, ndi miyoyo ya anthu.

Satana amatseka maso a okhulupirira ndikulimbana nawo mmagawo a kulambira, Mawu, mayendedwe awo a tsiku ndi tsiku, ndi kagwiridwe kayo ka tchito ndi Mulungu. Nkhondo imachitikanso mu matupi anu pamene Satana amabweretsa matenda otsiyanasiyana.

MMNENE NKHONDOYI INAYAMBIRA

Nkhondo yotsaonekayi inayambira kumwamba ndi ngelo otchedwa Lusifa yemwe anali ngelo okongola olengedwa ndi Mulungu. Lusifa amafuna kutenga Ufumu wa Mulungu. Munthu kuwerenga za kupandukaku pa Yesaya 14:12-17 ndi Ezakieli 28:12-19. Gulu la angele linamusata Lusifa (yemwe pano amatchedwa Satana) mukupanduka. Lusifa pamodzi ndi angelo opanduka anagwetsedwa kuchokera Kumwamba ndi Mulungu.

Ndipo munali nkhondo m'mwamba. Mikayeli ndi angelo ace akucita nkhondo ndi cinjoka; cinjokanso ndi angelo ace cinacita nkhondo. (Cibvumbulutso 12:7)

Ndipo cinaponyedwa pansu cinjoka cacikuru, njoka yokalambayo, iye wochedwa mdierekezi ndi Satana, wonyenga wa dziko lonse; cinaponyedwa pansu kudziko, ndi angelo ace anaponyedwa naye pamodzi. (Cibvumbulutso 12:9)

Lusifa anayamba kitchedwa kuti Satana ndipo angelo omwe anamutsata muupandu ngati ziwanda. Ziwanda zitha kulowa, kuzunza, kulamulira ndi kugwiritsa ntchito anthu omwe ali mu Ufumu wa Satana. Zimalimbikitsa kachitidwe koipa komwe kamachitidwa ndi anthu. Satana amatsogolera ziwanda zake mu kachitidwe kawo koyipa. Pamodzi ndi mphamvu zakumidimazi amalimbana ndi mtundu wa anthu.

CHIFUKWA CHIMENE KULI NKHONDO

Munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu ndi muulemerero wa Mulungu (Genesis 2). Nkhondo yosaoneka inayamba ndi yetsero loyamba mmunda wa Edeni (Genesis 3) pamene Satana anamuyetsa Adamu ndi Hava kuti akachimwe. Izi zinapangisa kuti munthu azibadwa ndi chikhalidwe cha uchimo ndi kumapanga uchimo chifukwa cha chikhalidwechi:

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12)

Komanso zinayambisa nkhono yosaoneka yapakati pa munthu ndi mphamvu yakumidima:

Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe (Satana) ndi mkaziyo (mtundu wa anthu), ndi pakati pa mbeu yako (mphamvu yakumidima) ndi mbeu yace (mphamvu ya bwino yoyimiridwa ndi Yesu) ... (Genesis 3:15)

Chifukwa cha tchimo, munthu analekanitsidwa ndi Mulungu naweluzidwa ku imfa. Imfa iyi inali imfa ya kuuzimu ya kulekanitsidwa ndi Mulungu. Inalinso imfa ya kuthupi, chifukwa pamene munthu anachimwa Satana analowa m'thupi la munthu nayamba kuyambisa matenda. Koma Mulungu anaconda munthu kwambiri ndipo anapanga ndongosolo lapaderadera lopulumutsa munthu ku tchimo:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi koteru, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.

Pakuti Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi iye. (Yohane 3:16-17)

Pakudzera mu chikhulupirira mwa Yesu, kuvomeredza ndi kulapa tchimo, amuna ndi akazi atha kuchotsedwa ku mphamvu ya woyipayo. Imfa ndi kuuka kwa Yesu sikunangobweretsa chipulumutso ku tchimo, inaonongaso oyipayo, Satana.

... Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi. (1 Yohane 3:8)

Koma ngati Satana anaonongedwa, bwanji nkhondo ikupitirirabe? Ndichifukwa chani timaonabe zoyipa paliponse? Ndichifukwa chani timayetsedwa ndi tchimo ndi matenda?

Ingakhale Yesu anagonjetsa Satana, tikukhala mu dziko lomwe ladzadzidwa ndi mphamvu ya mdierekezi. Kumvetsetsa njira zomenyera nkhondo ya uzimu zimatioasa ife kuthekera kothana ndi mdierekezi.

Satana akuyetsetsa kuika anthu mu ukapolo wa tchimo. Mukudzera mu njira zachinyengo akukopa anthu kukakhala moyo wa uchimo. Cholinga chake ndikufikira moyo ndi mzimu omwe ziri zake za Mulungu. Kumanso amafikira thupi ndikuligonjetsa ndi matenda:

Siikudza mbala (Satana), koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga, Ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Satana amafunitsitsa kukhala olamula wankulu. Akumenya nkondo yolimbana ndi thupi, moyo, ndi mzimu wa munthu. Njira zake zikulunjika pa Mulungu, mapulani anke ndi Anthu ake.

TANTHAUZO LA NKHONTHO YA UZIMU

Nkhondo ya uzimu ndi kusanthula kwa ndi kutengapo mbali pa nkondo ya uzimu yosaoneka. Imakamba za kumphunzira za mphamvu zotsutsana zabwino ndi zoipa, njira za satana, ndi njira za uzimu zogonjetsera woyipao.

Nkhondo yauzimu iposa kungosanthula mfundo za uzimu. imakamba za kutengapo mbali mu nkondo pa kuonetsera njirazi mu moyo ndi utumiki. Mwa imodzi mwa njira za Satana ndikutsunga okhulupirira kuti akhale osazindikira zida zake. Paulo anati ndikwabwino kuziwa njira za Satana...

kuti asaticenierere Satana; pakuti sitikhala osadziwa macenjerero ace. (2 Akorinto 2:11)

tikuyenera kuphunzira mmene tingathere za njira za Satana. Tikuyeneranso kuzindikira za chigonjetso pa Satana ndi mphamvu za kumidima. Tinayitanidwa ku ankhondo anzeru.

Kuzndikira nkondo ya uzimu ndikofunikira kwambiri:

Mukuyenera kudzikira kuti nkondo zonse zamoyo, kaya zathupi, zauzimu, maganizo, zachuma kapena za chikhalidwe cha munthu ndi zionetsero zazomwe zomayambitsidwa ndi nkondo ya uzimu.

Ingakhale mu dziko lakuthupi mabvuto atha kumaoneka ngati akuchitika chifukwa cha zochitika za moyo, nkondo zaku thupi zimayambira mu dziko la uzimu. Werengani nkhani ya Yobu yomwe ikutsimikidza mfundoyi (Yobu 1-2).

Tayesera kuthana ndi zoyipa zapa dziko lapansi kudzera ku mankhwala, maphunziro, malamulo, ndi zinthu zamakono. Koma izi sizinatheke chifukwa zoyipa zomwe tikuziona zimachokera ku zochitika za uzimu. Sizingathetsedwe ndi njira za kuthupi.

KODI NDINU AUFUMU UTI?

Mu dziko lakuthupi mfumu ndi amene amalamulira ufumu. Malo ndi anthu onse amuufumuwo amakhala ake. Amakhala ndi mphamvu ya moyo ndi imfa pa anthu ake. Izonso ndizoona mu dziko la uzimu. Inu muli mu Ufumu wa Mulungu kapena mu Ufumu wa Satana. Mulungu kapena Satana ali ndi mphamvu pa inu.

Imodzi mwa mafanizo okambidwa ndi Yesu amaonetsera kuti anthu amakhala mu Ufumu wa Satana kapena Ufumu wa Mulungu. Yesu anafanidzira dziko ndi munda. Mbeu za bwino

mmunda ndi ana amu Ufumu wa Mulungu. Mbeu zoyipa, yzomwe zimakula nakhala namsongole, ana a woipayo.

Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi namsongole ndiye ana a woipayo. (Mateyu 13:38)

Anthu amalowa mu Ufumu wa Satana pakudzera kubadwa mwa thupi. Baibulo limaphunzisa kuti anthu onse anabadwa mu uchimo. Izi zikutanthauza kuti ali ndi chikhalidwe cha tchimo kapena “mbeu” ya tchimo mwa iwo. Chokhumbakhumba chawo ndikupanga uchimo:

Onani, ndinabadwa m'mphulupulu: Ndipo mai wanga anandilandira m'zoipa. (Masalmo 51:5)

Kuti, mongaucimo unacita ufumu muimfa, comweconso cisomo cikacite ufumu mwa cilungamo, kufikira moyo wosatha mwa Yesu Kristu Ambuye wathu. (Aroma 5:21)

Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu. (Aroma 3:23)

Chifukwa choti tinabadwa ndi chikhalidwe cha uchimo, tinakhalapo mbali ya Ufumu wa Satana. Onse omwe amakhalabe ochimwa amakhalabe mbali ya Ufumu wa Satana. Uthenga wonse wa Mawu olembedwa a Mulungu, Baibulo, ndi dandaulo kwa munthu kuti achoke mu Ufumu woyipawo ndikupita mu Ufumu wa Mulungu. Anthu amabadwa mu Ufumu wa Satana pakudzera kubadwa kwa thupi. Akuyenera kuti abadwense mu Ufumu wa Mulungu kudzera mukubadwa kwa uzimu. Kulowa mu Ufumu wa Mulungu ndi kudzera mu kubadwanso mwatsoano komwe kwafotokozeredwa pa Yohane 3.

Pali kuyinana kuwiri kokha mu nkhondo yosaoneka. Yesu anati, “Iye wosabvomerezana ndi Ine atsutsana ndi Ine” (Luka 11:23). Inu simungakhale pakatikati mu nkhondo iyi. Inu muli mbali ina kapena inayo. Okhulupirira ena, chifukwa cha mantha akulimbana ndi Satana, amayetsera otsaganizira za nkhondo ndikupanga ubale ndi oyipayo. Amaganidza kuti akakhala kuti sakulimbana ndi Satana, iye salimbana nawo. Iyi ndi njira yayikulu ya Satana. Amyetsetsa kupamgitsa kuti ankhondo a Mulungu akhale osachitachita.

Koma palibe malo apakatikati. Inu ndinu ogonjetsedwa kapena ogonjetsa. Inu mukhala ogonjetsa mu thupi, moyo, ndi mzimu wanu kapena mugonjetsedwa, mupatsidwa ulesi ndi kukhumudwitsidwa. Inu mukhala ogonjetsa mu thupi lanu kapena mukhala ofokoka ndi odwaladwala. Kodi mukhala kuti?

Kuyitana kwa uzimu ku nkhondo kukupitirirabe. Kodi muli ku mbali ya Mulungu kapena Satana? Kodi muli mu Ufumu wa Satan kapena Ufumu wa Mulungu? Kodi inu ndi wa ufumu uti? Kodi inu ndinu ogonjetedwa kapena ogonjetsa mu nkhondo yosaoneka?

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Kodi zigawo ziwiri zimene zakambidwa pa 1 Akorinto 15:44-49 ndi ziti?

3. Lemabani ma ufumu awiri osaoneka a mu dziko.

4. Lembani mphamvu za uzimu za oyipayo.

5. Lembani mphamvu za uzimu zabwino.

6. Tanthauzirani mawu oti “mfumu”

7. Tanthauzirani mau oti “ufumu.”

8. Kodi “nkhondo ya uzimu” imatanthauza chani?

9. Kodi ndichifukwa chani kuti kulimbana mu uzimu?

10. Kodi mfundo zomvetsetsera nkhondo ya uzimu ndi chani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Baibulo limati “gwirani nchito yace ya cipulumutso canu ndi mantha, ndi kunthunthumira” (Afilipo 2:12). Machiritso ndi mbali ya chipulumutso yoperekedwa kudzera mu imfa ndi kuuka kwa Yesu Khristu. Mutha kufunsa, “ngati inaperekedwa kudzera mu imfa ya Yesu, nanga ndichifukwa chani tikuyenerfa kugwira ntchito”

Chikhulupiriro ndi ntchito zimayenda limodzi. Chikhulupiriro chopanda ntchiito ndi chakufa, komanso ntchito zopanda chikhulupiriro ziri chabe (Yakobo 2:17-26). Mukuyenera kukhala ochita Mawu osati akungomva okha.

Lonjezo la machiritso la phunziro iri likubvumbulutsa kuti mukuyenera kugwira ntchito ndi Mulungu mu gawo la thanzi lanu:

...Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoono pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)

Mu phunziro linalirilonse mu bukuli, gawo la **Kuchita mawu** ikutenga lingaliro lomwe laphunzidwa ndi kupereka mwayi kuti inu mukagwiritse ntchito chikhulupiriro chanu pa moyo wanu. Zimakuthandizani kuti mukakhale ochita Mawu osati ongomva chabe.

Gawo iri ndi gawo lofunika kwambiri paphunziro. Ngati mukudwala, yapangidwa kuti ikutengereni kumachiritso. Ngati mukutumikira kwa munthu yemwe akudwala, poyamba gawanani zomwe ziri mu phunziro ndi iwo akudwala ndipo malizitsani gawoli limodzi ndi iwo kuti muwatengere kuti akalandire machiritso.

2. Werengani nkhani ya Yesu ndi mkazi wa Suro-Fonika pa Marko 7:24-30. Nkhani iyi imabvumbulutsa kuti machiritso ndi “chakudya cha ana.” Izi zikutanthauza kuti machiritso ndi a ana a mu Ufumu wa Mulungu. Mulungu amachiritsa osakhulupirira mwa zifundo kuti awabweretse ku chipulumutso, koma machiritso ndi a ana Mullungu.

Ngati mukufuna machiritso, chochita choyamba ndikukhala mwana wa Mulungu. Mukuyenera kulapa machimo ndikulandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi ndi mchilitsi wanu. Ngati simunapange idzi, pempherani pemphero iri:

Ambuye, ndikudziwa kuti ndine ochimwa ndipo ndikudzindikira ndi kulapa machimo anga. Ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu wa moyo ndipo ndi njira, choonadi, ndi moyo. Ndikumvomeredza nsembe ya Yesu Khristu ndikukhulupirira kuti anafa chifukwa cha ine pa ntanda. Ndikhululukireni ndikundiweretsa ku machimo anga. Mu dzina la Yesu, Amen.

3. Madziko abwino a uzimu ndiofunika kuti tikamenye nkondo yopambana ya uzimu. ngati muli okhulupirira atsopano, pedzani phunziro la Harvestine International Institute lotchedwa “*Madziko a Chikhulupiriro.*”
4. Kodi inu mukumva kuti mwakhala ogonjetsedwa ku nkondo yosaoneka? Kodi ndi mbali iti ya woyo kapena utumiki wanu mwakhala mukugonjetsedwa? Kodi mwakhala mukugonjetsedwa mu

- ___Mu dziko lauzimu?
- ___Mu dziko lamaganizidwe?
- ___Mu dziko la kuthupi?

Pomwe mukuphunzira bukuli, muphunzira njira zokuthangatirani mu magawo amenewa.

5. Onanitso nkhani yapa 2 Mafumu 6 yomwe yakambidwa mu phunzirori. Kodi mukudziwa anthu ngati Gehazi kapena omwe ali mu mzinda wa Dotani omwe sakudziwa kapena ali ndi mantha a nkondo ya Satana pa matupi awo? Kodi inu mungawathandidze bwanji?
-
-

6. Poti nkondo ya uzimu iri ndi zigawo zambiri, inu mutha kumenyana ndi ntchimo painu nokha, kapena kuthana ndi zoipa za padziko lapansi, ndi kapena kudzera mu utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe. Yambani kupempherera gawo lanu la nkondo ya uzimu. ngati simukudzindikira nkondo ya uzimu, werengani mu phunziro la Harvestine International Institute lotchedwa “*Njira za Uzimu: Buku la Nkondo ya Uzimu.*”
7. Werengani Baibulo lonse ngati buku la nkondo ya uzimu. muli nkhani za nkondo ya uzimu, kupambana ndi kugonjetsedwa kwa nkondo zakale. Komanso imakamba za uneneri, kubvumulutsa nkondo za uzimu za mtsogolo mpakana kufikira nthawi ya nkondo yomaliza.

CHAPUTALA 2

KUYITANA KU ZIDA ZA NKHONDO

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kudzindikira mawu otsiyanatsiyana ogwiritsidwa ntchito pa machiritso.
- Kutanthauza machiritso auzimu.
- Kutsiyanyitsa pakati pa machiritso ndi kumasula.
- Kufutokoza momwe machiritso ndi kumasula zmakhudzana ndi ntchito yokafikira dziko ndi Uthenga Wabwino.

LONJEZO LA MACHIRITSO

Ndipo muzitumikira Yehova Mulungu wanu, potero adzadalitsa cakudya cako, ndi madzi ako; ndipo ndidzacotsa nthenda pakati pa iwe. (Eksodo 23:25)

CHIYAMBI

Mu Chipangano Chakale lipenga limagwiritsidza ntchito pofuna kuyitanira anthu a Mulungu ku nkondo. Lero, kuitana kwa uzimu kukuchitika pa dziko lonse lapansi. Ndi kuitana ku nkondo yosaoneka. Ndikuitana ku zida za nkondo. Phunziro iyi ikuyitana inu kuchokera ku moyo wogonjetsedwa ndi ukapolo ku moyo wa chipambano ndi mtendere mwa Yesu Khristu.

TANTHAUZA LA MACHIRITSO

Pali mawu ambiri omwe agwiritsidwa ntchito ngati mawu akuti kuchiritsa:

Kuchiritsa kwamaganizo: Mawu awa amagwiritsidwa pofotokoza machiritso a maganizo pa chinthu, ufiti, zinthumwa, ndi zamizimu zomwe sizili za m’Baibulo.

Machiritso auzimu: Pali magwero ena a machiritso auzimu omwe sachokera kwa Mulungu, ndiye sitigwiritsa mawu awa mu phunziro lathu. Satana atha kupanga machiritso auzimu (Eskodo 7:8-13).

Machiritso akuchipatala: Mtundu uwu wa machiritso umagwiritsidwa ndi madotolo, anamwino, kuzipatala, ndi makhwala. Pomwe tikhala tikuphunzira, njira yovomerezeka simatsutsana ndi Mawu a Mulungu kapena machiritso aumulungu, koma ndikutambasuka kwa ubwino wake.

Machiritso achilengedwe: Machiritso omwe amachitika kudzera mumatupi a anthu popanga chithandizo chirichonse chakuchipatala. Izi zimaonetsera khalidwe la Mulungu ndi ntcito yake mumatup a anthu. “Machiritso achirengedwe” amakambatso zakugwiritsa ntchito njira zachirengedwe monga chakudya chabwino, mavitamini ndi mchere wachirengedwe, kupuma kokwanira, ndi zina zotero.

Machiritso a chikhulupiriro: Mawu awa amagwiritsidwa ntchito pokamba za machiritso a Mulungu. Sitirigwiritsa ntchito, komabe, chifukwa limalanjika ku chikhulupiriro cha iye akutumikira kapena akulandira utumiki.

Machiritso aumulungu: Mawu oti “umulungu” limalunjika kwa Mulungu, osati chikhulupiriro cha munthu. Komanso imatsiyansidwa ndi zamatsenga ndi machiritso auzimu. “Umulungu” umakamba za Mulungu woona ndi chikhalidwechake, chomwe chimaonetsedwa mu Mawu Ake, Baibulo.

Mu phunziro iri tiphunzira mawu oti “machiritso aumulungu.” Machiritso aumulungu ndi pamene Mulungu waonetsera ukulu wake, malonjezano ake, ndikugwira ntchito pa moyo wa munthu pakumchiritisa iye mu thupi, moyo, ndi mzimu.

Machiritso aumulungu antha kuchitika pa nthawi yomweyo kapena mwapang’onopang’ono. Ingakhale mmachiritso anthawi yomweyo amaonetsera kupezeka kwa Mulungu ndi mphamvu ya Mulungu, machiritso omwe amachitika pang’onopango’no sikuti simachiritso aumulungu (onani Marko 8:22-255). Machiritso a kuchipatala ndi achilengedwe nawonso atha kutengedwa ngati machiritso aumulungu, chifukwa ndi Mulungu amene amabweretsa machiritso.

MACHIRITSO NDI MAMASULIDWE

Tigwiritsa ntchito mawu oti “machiritso” ndi “mamasulidwe” mosinthana mu phunzirori. Machiritso amatumikiridwa ku matenda aku thupi ndi maganizidwe pomwe mamasulidwe amathana ndi matenda oyambitsidwa ndi ziwanda.

Pamene mukuphunzira ponzirori, chifukwa munthu ndi thupi, soyo ndi mzimu, matenda aziwanda omwe akuza ubongo atha kufalikira ku thupi lonse. Matenda athupi atha kuyambitsa matenda a ziwana amu ubongo. Ndiye ingakhale machiritso ndi mamasulidwe ndiwosiyana, komanso amafanana chifukwa chachikhalidwe cha munthu.

KUYITANA KU ZIDA ZA NKHONDO

Mpingo woyamba unkaona zichitochito zawo za uzimu ngati nkondo ya uzimu. Mawu a nkondo agwiritsidwa mu Chipangano chonse Chatsopano. Chitetedzo chiri mu zida a nkondo za Mulungu. Mawu a Mulungu akufaniziridwa ndi lupanga. Machenjerero atsatana akutchedwa mibvi. Chikhulupiriro ndi kumenyana kwabwino ndi okhulupirira akuuzidwa kuti amenye nkondo yabwino ya uzimu.

Moyo wachikhristu ndi nkondo. Satana aptirira kulimbana ndi moyo ndi mzimu wa munthu. Amachenjereranso thupi la munthu ndi matenda ndi ukapolo. Mulungu akuyitanira anthu ake ku nkondo yochenjera. Kuyitanaku kukupita kwa ophunzir kuti azitengere iwo okha zida za Mawu a Mulungu ndikutenga machiritso ndi mamasulidwe ku m’badwo uno.

Mu Chipangano Chatsopano, Yesu satume aliyense kukalalikira Uthenga Wabwino opanda osawalamulira kuti akatumikira machiritso ndi mamasulidwe. Anawauza kuti “Pomwe mukupita ... kachiritsemi, odwala kutulutgsa ziwanda...” (Mateyu 10,1,7-8)

Pomwe anthu ochuluka anabwera kuzachiritsidwa ndi kumasulidwa, kukolola kwa uzimu kunayamba kuchuluka mpaka ogwira ntchito ena anayamba kufunidwa. Sipanapite nthawi pomwe ophunzira 72 ena anafunidwa ndipo anatumizidwa kukalalikira, kuphunzisa, kuchilitsa ndi kumasula.

Pali njira zambiri zatsopano zomwe zingathandidze pakufalitsa Uthenga Wabwino. Izi zimatchedwa kuti “luso lazayansi.” Zimaphatikidza zinthu monga malo osindikizira mabuku, makina a kompyuta, wailesi zonvera ndi za kanema, zomvetsera ndi zoonera. Njira zatsopano zakayendedwe zimathandizanso anthu kuyenda mofulumira kukafalitsa Uthenga Wabwino. Luso la sayansi ndilofunikira kwambiri koma mphanvu ya Uthenga Wabwino ndiya nkati. Mwa ichi tikutanthauza kuti mphanvu ili mu Uthenga Wabwino. Ichi ndi chimwene fanizo la chotupitsa ndi la mbeu ya mpiru likunena.

Ndiponso anati, Ndidzafanizira Ufumu wa Mulungu ndi chiani? Ufanana ndi chotupitsa mikate, chimene mkazi anatenga, nachibisa mu miyeso itatu ya ufa, kufikira unatupa wonsewo. (Luka 13:20-21)

Ndimeyi ikusonyeza kuti ntchito ya Mulungu simapita patsogolo chifukwa cha kufuula ndi kulengeza. Mutha kumayembekezera kuti Ufumu wa Mulungu ufalitsidwa kudzera munjira za nkondo pogonjetsa mayiko ena. Koma kufalitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu kuli nagti chotupitsa mu mkate. Chotupisa chitha kukhala chaching’ono komanso chobitsika, koma chiri ndi kuthekera kopanda malire. Ngati chotupitsa, mphanvu ya Ufumu siyakunja koma yankati mwa munthu.

Mu chitsanzo china, Yesu anayerekeza kufalitsidwa kwa Ufumu wa Mulungu ndi ka mbeu kampiru

Pamenepo ananena, Ufumu wa Mulungu ufanana ndi ciani? ndipo ndidzaufanizira ndi ciani?

Ufanana ndi kambeu kampiru, kamene munthu anatenga, nakaponya m'munda wace wace, ndipo kanamera, kanakula mtengo; ndi mbalame za m'mlengalenga zinabindikira mu nthambi zace. (Luka 13:18-19)

Mofanana ndi m'momwe chotupitsa chimafalikira, ka mbeu ka mpiru kamodzi kamakula ndikukhala ntengo waukulu. Chitsanzo chimenechi chimasonyeza mwa chete, koma ndi njira yamphanvu yopititsa patsogolo Ufumu wa Mulungu.

Mu fanizo lina, Yesu anati palibe chosatheka ngakhale ndichikhulupiriro chochepa ngati ka mbeu ka mpiru. Izi zikuonetsera kuti kufalitsidwa kwa Uthenga Wabwino suchepesedwa ku malo komwe kulibe luso la sayansi. Ngakhale ndichikhulupiriro chochepa, Ufumu wa Mulungu upitabe patsogolo. Kukolola kwakukulu kwa uzimu mu mbiri ya Mpingo ikukhalabe kuti itsonkhetsedwe. Ngati nthawi ya Chipangano Chatsopano, ikololedwa pakudzera pa kuwonetsera kwa mpamvu ya Mulungu mu kuchiritsa ndi mamasulidwe. Ichi ndichifukwa chake Paulo anati:

Ndipo mau anga ndi kulalikira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu;

kutichikhulupiriro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)

Pamene anabwerera kumwamba, Yesu anawapatsa okhulupirira udinndo ofalitsa Uthenga Wabwino ku mitundu ya dziko lapansi:

...Mukani ku dziko lonse lapansi, lalikirani Uthenga Wabwino kwa olengedwa onse. (Marko 16:15)

Simungakwanitse udindowu opanda ulamuliro. Yesu anawapatsanso omutsana ulamuliro kuti akakwaniritse ulamuliro. Ulamulirowo umakamba za mphamvu yomwe iri pa mwamba pa mphamvu zonse za Satana:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Kodi ndinu okonzeka kuyankha kuyitana kwa uzimu kaku nkondo ndikuchoka ku moyo wa matenda ndi magoli kupita ku moyo wa chipambano mwa Yesu Khristu? Kodi ndinu okonzeka kutumikira mu utumiki wakuonetsera mphamvu ya Mulungu? Kodi ndinu okonzeka kukamenya nkondo ya kuthupi? Kodi mukufuna mutaona odwala kuchilitsidwa ndi onse anali omangidwa ndi ziwanda akumatsulidwa? Uwu ndi utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe. Uwu siwa azitsogoleri a mipingo. Siwa azibusa kapena ma avangeli. “Zizizndikiro izi zidzawatsata iwo okhulupirira.?”

Kodi ndinu okhulupirira? Ngati muli chonch, inunso, mukuyenera kuyankha muyitano waku zida za nkondo.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Tanthauzirani mawu otsatirawa omwe akugwiritsidwa ntchito pa machiritso.

Kuchiritsa kwamaganizo:

Machiritso auzimu:

Machiritso akuchipatala:

Machiritso achilengedwe:

Machiritso a chikhulupiro

3. Tanthauzirani machiritso aumulungu.

4. Kodi kusiyana kwapakati pa machiritso ndi mamasulidwe ndi chani?

5. Kodi machiritso ndi mamasulidwe akukhuzana bwanji ndi ntchito yofikira dziko lonse ndi Uthenga Wabwino

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. **Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)**

Kodi ndinu okhuluoirira?

Ngati ziri chonco, kodi zizindikiro zikukutsatani? Kodi odwala akuchiritsidwa ndi iwo omwe akhuzidwa ndi ziwana akumasulidwa?

Ngati ayi, kapamphereni pomwe mukuwerenga bukuli Mulungu atsedula mtima wanu kuti mulandire utumiki uwu wa machiritso ndi mamasulidwe zomwe ziri zanu.

2. Ngati ndinu abusa, mvangeli, kapena mphunzitsi, onani mawu awa:

Ndipo mau anga ndi kulalikirira kwanga sanakhala ndi mau okopa a nzeru, koma m'chionetso cha Mzimu ndi cha mphamvu; kutichikhulupiriro chanu chisakhale m'nzeru ya anthu, koma mu mphamvu ya Mulungu. (1 Akorinto 2:4-5)

Kulalikirfa kapena kuphunzisa kopanda mphamvu kumapangitsa kumalankhula “mau okopa a nzeru za anthu” ndi kulimbikitsa chikhulupiriro pa munthu osati Mulungu. Taganizirani Paulo kumayang'ana m'malemba zitsanzo za anthu pa uthenga wake? Taganizirana iye ankukamba nkhani zotseketsa za zomwe zinachitika ku Atena ndi Korinto? Tamuoneni akuyambitsa gulu lochita zitsuzo? Paulo anazindikira kuti si mawu okopa, mzeru za munthu, kapena zisunzo zomwe zimabweretsa anthu kwa Mulungu. Zinali kuonetsera Mzimu ndi mphamvu. Kodi utumiki wnu uli pati?

3. Kodi mukufuna machiritso kapena mamasulidwe? Onaninso tanthauzo la machiritso:

“Machiritso aumulungu ndi pamene Mulungu waonetsera ukulu wake, malonjezano ake, ndikugwira nchito pa moyo wa munthu pakumchiritsa iye mu thupi, moyo, ndi mzimu.”

Pemphero lathu pa inu ndiroti musanamalize phunzirori, Mulungu akhala kuti wabvumbulutsa chikhalidwe chake, kukwaniritsa malonjezano ake, ndipo inu muchiritsidwa mu thupi, moyo, ndi mzimu wanu.

CHAPUTALA 3

NKHONDO ISANAYAMBE

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kelemba mayankho anayi a machiritso ndi mamasulidwe
- Kulemba mwachiduwe machenjezo operekedwa ka azitsogoleri omwe satumikira machiritso.
- Kufotokoza kufunikirakwa chiphunziso cha machiritso ndi mamasulidwe.

LONJEZO LA MACHIRITSO:

Mwananga, tamvera mau anga; Cherera makutu ku zonena zanga. Asacoke ku maso ako; Uwasunge m'kati mwa mtima wako. Pakuti ali moyo kwa omwe awapeza, Nalamitsa thupi lao lonse. Cinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; Pakuti magwero a moyo aturukamo. (Miyambo 4:20-23)

CHIYAMBI

Musanayambe kuphunzira machiritso ndi mamasulidwe ndikwabwino kuti mumvetsetse makhalidwe omwe mungakumane nawo pamene mukuyamba kutumikira mu madera amenewa. Pankhani ya machiritso ndi mamasulidwe, okhulupirira ambiri ama:

NYALANYAZA:

Muthu wina ochita maphunziro azumulungu anawunikira ma tsamba 87,125 azolemba zaumulungu mu malo otsungira ma buku a sukulu evangeriko. Mwamatsamba onsewa, panali matsamba 71 okha omwe amakamba za machiritso, matsamba 131 za zozizwitsa, ndi matsamba 85 okamba za zizindikiro ndi zodabwitsa. Pomwe ma vesi ochuluka a Chipangano Chatsopano okamba za phunzirori akayerekezedwa ndi matsamba ochepa omwe alembedwa kukamba za nthaniyi pa maphunziro azaumulungu matsiku ano, timaona chizolowezi chonyalanyaza phunzirori mu masukukulu a ma evangeriko.

Ena amanyalanyaza za machiritso chifukwa cha machenjezo a m'Baibulo okhuza zozizwitsa zonyenga. Iwo amatenga ichi kukhala chenjezo cha zozizwitsa zonse (Marko 13:22-23). Ena makhulupirira machiritso muzolemba zokha, koma amanyalanyaza powachita. Ena amanyalanyaza chifukwa sangayankhe mafunso onse okhuzana ndi matenda. Ena amanyalanyaza machiritso chifukwa cha mantha oti mwina atha osakwanitsa. Zikuoneka kuti timakhala ndi mapanga awiri. Timapemphera molimbika mtima pofuna zachuma, nzeru, ndi chitsogozo kuma timakhala ndi mantha kupempherera machiritso.

KUWAKANA:

Ena amakana machiritso ndi mamasulidwe kuti ndi alero chifukwa alibe chiphunziso, chitsanzo, kapena sizinawachitkirepo iwo.

Mu Chipangano Chatsopano muli nkhani 26 zokkhuza machiritso. Buku la Machitidwe muli zisanu. Machiritso akuthupi akambidwa pa 1 Akorinto 12:8-11 ndi 28-30. Yakobo 5:13-16 pali malangizo a momwe mungapempherere munthu odwala. Palibe pomwe amakweza machiritso a mu chiphunzitsa chamu Uthenga Wabwino. Kupempherera odwala zimatengedwa zopanda phundu kwambiri pa nthawi imene Makalata amalembedwa, ndipo palibe choonetsa kuti machiritso aumungu anali otsutsidwa mu mpingo wakale.

KUWAVUTISA:

Anthu ena avutitsa machiritso ndi mamasulidwe ndi chikhaledwe cha anthu comwe ziri zosiyana ndi Mau a Mulungu. Muphunzira mwazina zazikhalidwezi mu chaputala 11. Ena ayivutitsa ndi zomwe akumana nazo. Atha kuti amapempherera machiritso ndipo sanalandire. Koma inu muyike chikhulupirriro chanu pa Mau a Mulungu, osati zokumana nazo (pokhapokha zokumana nazo zikugwirizana ndi Mau a Mulungu).

KUCHEDWETSEDWA:

Anthu ena amachedwetsa kutumikira machiritso ndi mamasulidwe chifukwa alibe mayankho achinachirichonse. Samamvetsetsa chifukwa chimene ena amachiritsidwa ena ayi. (muohunzira za izi mu chaputala 13). Ndiichotsafunikira kuti mumvetsetse kaye chinachirichinse chokhudzana ndi machiritso kuti mutumikire kapena kulandira.

Maynkho ena amabwera pamene mukutumikira ndi kukumana ndi mphamvu ya Mulungu ya machiritso. Mafunso ena sazayankhidwa. Ngati munakakhala kuti mukuziwa chinachiri chonse ndiye simunakamufuna Mulungu. Baibulo limati “timaziwa pang’ono chabe.” Machiritso amakhuza matenda ndi mavuo ndipo nthawi zonse pazakhala zinsinsi chifukwa zisisi za kusawerezika zikugwira ntchito (1 Atesalonika 2:7).

KUFUNIKIRA KWA CHIPHUNZITSO CHABWINO

Kuunikira kwa maganizo omwe alipo pa za machiritso ndi mamasulidwe zikuonetsera chifukwa chimene tikufunikira chiphunzitsa chabwino pa phunzirori. Athu ambiri akuonongeka kuthupi ndi kuuzimu chifukwa sakuziwa zimene Mau a Mulungu amaphunzitsa paza machiritso:

Anthu anga aonongeka cifukwa ca kusadziwa (Hoseya 4:6)

Machiritso (ungwiro) ndi mbali ya Uthenga Wabwino wa Ufumu omwe tapansidwa ntchito yoti tiwufalitse (Luka 16:15-18). Yesu anatiyitana kuti tikalalikire, kuphunzitsa, kuchiritisa ndi kumasura. Machiritso ndi mamasulidwe sakuyenera kusiyidwa, koma akuyenera kumatsindikidwa pamene tikulalikira ndi kuphunzitsa za Uthenga Wabwino. Baibulo limakamba kuti makachisi athu akuyenera kukhala malo amachiritso (Luka 14:16). Tikuyenera kuwona anthu akuchiritsidwa osati kuwabweza:

Ndipo lambulani miseu yolunjika yoyendamo mapazi anu, kuti cotsimphinaco cisapatulidwe m'njira, koma ciciritsidwe. (Ahebri 12:13)

Ngati okhulupirira, ndi nchimo ngati sitigawa uthenga wabwino wa machiritso ndi mamasulidwe kwa otayika ndi dziko lomwe likufa. Baibulo likuta:

...kwa iye amene adziwa kucita bwino, ndipo sacita, kwa iye kuli cimo. (Yakobo 4:17)

kuziwa kuti tinalamuliridwa kuti tikatumikire machiritso—koma osachita—ndi tchimo. Mulungu anapereka machenjezo okhwima kwa adzitsogoleri omwe satumikira machiritso:

...Tsoka abusa a Israyeli odzidyetsa okha... Zofoka simunazilimbitsa; yodwala simunaiciritsa, yotyoka simunailukira chika, yopitikitsidwa simunaibweza, yotayika simunaifuna; koma munazilamulira mwamphamvu ndi moopsa, Ndidzafuna yotayika, ndi kubweza yopitikitsidwa, ndi kulukira chika yotyoka mwendo, ndi kulimbitsa yodwalayo; koma yanenepa ndi yolimba ndidzaziononga, ndidzazidyetsa ndi ciweruzo. (Ezekieli 34:2,4,16)

KUYAMBA NDI KAGANIZIDWE KABWINO

Pomwe mukuphunzira phunziro la machiritso ndi mamasulidwe, mukuyenera kuchita izi ndi kaganizidwe kabwino. Nthawi zonse muzikumbukira kuti kufuna machiritso ndi zotsatira kwa chaiyanjanitso cha uzimu kudzera mwa Yesu Khristu chomwe chiri chozizwitisa chachikulu cha machiritso.

Pomwe mukuphunzira mukuyenera kusiya zimphunzitso zonse za chikhalidwe acha anthu zomwe munaphunzira. Mukuyenera kukhala oti mutha kuphunzitsidwa. Chimodzi mwa zizindikiro za nzeru kuchokera mwambamu ndichakuti chikupereka mpata oganiza (Yakobo 3:17). Inu muli pachiopezo ngati simukhala ophunzitsidwa. Kumbukirani kuti tchimo longoganizira ndi kuyika Mulungu mu “khungu” lanu. Abwenzi a Yobu anachimwa mwa njira iyi.

Muyambe kuphunzira phunziro iyi ngati kuti simunamveko za ziphunzitso za chikhalidwe cha anthu ku mipingo yanu. Vomerezani chomwe Mau a Mulungu akunena. Ngati akunena kuti ndinu ochiritsidwa, khulupirirani. Ngati akunena kuti muyike manja anu pa odwal, chitani.

Musaphunzire phunzirori ndicholinga chosaka nmitundu kapena njira zolandirira kapena kutumikira machiritso. Baibulo siripereka njira yeniyeni, ingakhale mfundo zosiyanasiyana zabvumbulutsidwa ndipo tizona. Mmalo mumasaka njira, mvetsetsani kuti ochiritsa ali nkati mwanu. Funani kukulitsa chidziwitso chanu ndi ubale wanu ndi Iye.

Yesu ndi Mzimu woyera akukhala mwa inu. Machiritso chi chinthu chomwe mumakasaka kunja, koma ndi chinthu chomwe mumaphunzira kutulusa kuchokera mkati mwanu. Inu mukufuna kuti mumvetsetse mfundo zomwe zimatulus mphamvu yomwe imakhala mwa inu.

UTUMIKI WA MACHIRITSO

Musanayambe utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe zindikirani kuti ngati mukutsatadi chitsanzo cha utumiki wa Yesu wa machiritso ndeukti inu mu:

-Muzakhala kapolo osati “mbuye”: Marko 10:44

-Kulema, osati kulemera: Marko 6:31; Yohane 4:6; Machitidwe 3:6

-Kukumana ndikusakhulupirira kwa anthu ena: Marko 13:58

-Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa atsogoleri achipembedzo: (Ena mwa iwo alingati Afalisi... amene amakhala okhudzika kwambiri ndi chilamulo ndi makhalidwe amoyo): Luka 6:6-9

-Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa amene akuyandikirani: Marko 6:4 ndi Mateyu 13:58

-Kupewa kulengeza malo moyisaka: Marko 8:36; Mateyu 8:4

-Kukana kufuna kupindula inu eni kapena kupeza zinthu kupyolera mu mphamvu ya Mulungu: Machitidwe 8: 18-24

-Kukana kupatsidwa ulemu: Machitidwe 14:8-18

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Lembani mayankho anayi omwe amaperekedwa ku machiritso ndi mamasulidwe.

3. Lembani mwachidule machenjezo oomwe aperekedwa ku adzitsogoleri omwe satumikira machiritso.

4. Ndichifukwa chani maphuziro a machiritso ndi mamasulidwe akufunika?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Fufuzani malingaliro omwe muli nawo pa machiritso. Onani omwe akugwira ntchito. Kodi inu:

_____mwawanyozetsa?

_____Mwawakana?

_____Mwawavutitsa ndi zikhalidwe za anthu ndi zokumana nazo

_____Mwayichedwetsa

2. Lembani dongosolo la momwe mungakonzere malingaliro anu

3. Ngati muli tsogolere wa uzimu, kodi mwakhala mukulalikira, kukhunzitsa, ndi kutumikira machiritso mowirikiza? Ngati ayi, lembani dongosolo lokonza izi:

4. Ngati mukutumikira kale machiritso, kodi utumiki wanu ukufanana bwanji ndi utumiki wa Yesu mu njira izi:

-Muzakhala kapolo osati “mbuye”: Marko 10:44

-Kulema, osati kulemera: Marko 6:31; Yohane 4:6; Machitidwe 3:6

-Kukumana ndikusakhulupirira kwa anthu ena: Marko 13:58

-Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa atsogoleri achipembedzo: (Ena mwa iwo alingati Afalisi... amene amakhala okhudzika kwambiri ndi chilamulo ndi makhalidwe amoyo): Luka 6:6-9

-Kukumana ndi chizuzo chochokera kwa amene akuyandikirani: Marko 6:4 ndi Mateyu 13:58

-Kupewa kulengeza malo moyisaka: Marko 8:36; Mateyu 8:4

-Kukana kufuna kupindula inu eni kapena kupeza zinthu kupyolera mu mphamvu ya Mulungu: Machitidwe 8: 18-24

-Kukana kupatsidwa ulemu: Machitidwe 14:8-18

5. Werengani lonjezo la machiritso la phunzirori:

Mwananga, tamvera mau anga; Cherera makutu ku zonena zanga. Asacoke ku maso ako; Uwasunge m'kati mwa mtima wako. Pakuti ali moyo kwa omwe awapeza,

Nalamitsa thupi lao lonse. Cinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; Pakuti magwero a moyo aturukamo. (Miyambo 4:20-23)

Mukuyenera ku:

- Kumvera Mawu a Mulungu.
- Kuchera makutu ku Mawu a Muungu.
- Kusunga Mawu Ache pa maso panga.
- Kuwasunga m’kati mwa mtima mwanga.
- Kuchingiriza mtima wanga kuposa zonse ndizizunga.

Mawu a Mulungu amakudzana ndi za umoyo. Malamulo ake akuti:

- Moyo kwa omwe awapeza.
- Nalamitsa thupi lawo lonse.

Muonenso pa vesi 23 ubale wa chkhaliidwe cha mtima ndi magwero a moyo.

6. Kudzindikira kuti Yesu ndiye magwero a machiritso oonadi aumulungu ndikofunikira kwambiri ndi kukula kwa zimene zikutcheda kuti m’badwo watsopano. M’badwo uwu umagwiritsa nchito njira za thupi ndikufuna chithandizo kuchokera ku mphamvu yauzimu yoyipa. M’badwowu umagwiritsa nchito mizimu, zaziamba zomwe zisali za m’Baibulo cholinga kufuna kupeza machiritso. Njira zimezezo zikuyenera kukadidwa chifukwa zimaswa Mawu a Mulungu.

GAWO LACHIWIRI

CHIWEMBU

Chiwembu ndi machitachita a mphamu ndi a chiwawa. Ntchimo ndi chiwembu cha Satana pa moyo ndi mzimu wa munthu. Matenda ndi chiwembu pa thupi la munthu.

Kuti mumenyane ndi chiwembu cha Satana pa thupi lanu, mukuyenera kuti mumvetsetse matenda. Mu gawo ino muphunzira

- **GWERO LA MATENDA**
- **ZIFUKWA ZA MATENDA**
- **MITUNDU YA MATENDA**
- **ZOTSATIRA ZA MATENDA**

CHAPUTALA 4

GWERO LA MATENDA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kufotokoze momwe matenda ndi imfa zinalowera mu dziko.
- Kudzindikira gwero la matenda.
- Kudzindikira zinthu zowononga za matenda.
- Kufotokoza momwe Mulungu amaonera matenda.
- Kufotokoza momwe mungamasukire ku temberero a matenda ndi imfa.

LONJEZO LA MACHIRITSO:

Kristu anatiombola ku temberero la cilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense woo paeikidwa pamtengo. (Agalatiya 3:13)

CHIYAMBI

Pali gwero limodzi la matenda, ingakhale pali zifukwa zosiyanasiyana zimene anthu madwalira. Paulo anatmikizira izi pomwe anati “Cifukwa cace ambiri mwa inu afoka, nadwala” (1 Akorinto 11:30). Chaputala ichi chikukamba za gwero la matenda ndipo Chaputala 5 chikufotokoza zifukwa za matenda.

MOMWE MATENDA NDI IMFA ANALOWERA MU DZIKO

Genesis 1 ndi 2 mu Baibulo imakamba nkhani ya kullengedwa kwa munthu. Mulungu analenda munthu mu chifaniziro Chake, ndikuuzira mpweya wa moyo mu m'mphuno zake, ndipo munthuyo anakhala wa moyo. Munthu analengedwa ndi zikhalidwe zitatu za thupi, moyo, ndi mzimu. Poyamba, mbali zonse za munthu zinali pa ubale ndi zina ziwiri, ndipo chikhalidwe chonse cha patatu unali pa ubale ndi Mulungu. Munthu anli opanda tchimo ndi wathanzi mu thupi, moyo ndi mzimu.

Genesis 3 imakamba momwe anthu oyamba, Adamu ndi Hava, ananchimwira Mulungu pakutsamvera Mawu Ache. Tchimo lawo linabweeretsa temberero la tchimo ndi imfa pa anthu onse:

Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; coteru imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. (Aroma 5:12)

Temberero la imfa linali kulekanitsidwa mu uzimu pakati pa munthu ndi Mulungu komanso imfa ya kuthupi yomwe imakhala chmalidziro cha moyo wa munthu pa dziko. Titha kuona zotsatira za temberero mu zolembedwa za mu Genesis. Adamu ndi Hava anabitsara kuopa Mulungu

chifukwa cha matenda a uzimu. Adamu anati Hava ndi amene analakwisa, chimene chiri chiyambi cha matenda a maganizo kuchokera ku ubale wosokonezeka. Kaini anapha Abele, chomwe chiri chitsanzo cha matenda a pachibale. Matenda a thupi analowa pomwe Sarah anali osabereka ndi mliri pa banja la Abileki.

SATANA NDIYE GWERO

Pamene temberero la imfa linabwera pa munthu, Satana analowa mu thupi lamunthu nayamba kuliononga. Baibulo limatsimikidza kuti Satana ndiye magwero a zoyipa pa dziko. Yesu anatindi mbala ndi ...

Siikudza mbala, koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi kuononga... (Yohane 10:10)

Matenda amaononga thupi ngati mmene tchimo liononga mzimu. Matenda amaba thanzi, chimwemwe, ndalama, nthawi, nchito, ndi mphamvu. Amaphazi ndi kuononga. Ngakhale “ngozi” zomwe zimaononga thupi ndi wothandizira a Satana. Chifukwa gwero la matenda ndi Satana, mukuyenera kuwakaniza ngati mmene mupangira ndi mayetsero ndi tchimo. Pamene mukukaniza mayetsero ndi tchim, mukufana nkondo ya uzimu yolimbana ndi Satana pa moyo ndi mzimu wanu. Mukamakazina matenda, mukumenya nkondo yolimana ndi Satana pa matupi anu.

ZINTHU ZOWONONGA ZA MATENDA

Nthenda iliyonse imachokera kutizilombo mmoyo. Monga mzimu apereka moyo ku thupi, Satana naye apereka moyo kutizilombo. Monga mchilengedwe chadziko, Mulungu anatenga chamoyo nachichulukitsa kuti chikabweretse moyo. Satana amasinthanitsa chabwino ndi choipa. Amabweretsa tizilombo, matenda nawachulutsa kuti akabweretse imfa. Uwu ndi “mzimu wazofooka” omwe umagwira tchito mthupi lanu pomwe mukudwala. Pamene mzimu woipa watulutsidwa, nthenda imafa thupi mwanu. pokhapokha ngati tizilombo tamoyo tilipo mthupi, nthenda imakhalanso ndikupitilizabe ntchito yake yoononga.

Ngakhale kuti nthenda iliyonse siyochokera kumizimu yaziwanda, matenda amapezeka m'dziko chifukwa cha satana. Mwachitsanzo inu mutha kuyamba kumva kuzizira chifukwa munayenda osavala chofunda munyengo yozizira. Ichi si kulimbana kwa Satana ku matupi anu, koma matenda omwe amabwera chifukwa chakuzizira alipo pa dziko chifukwa cha Satana. (Inu muthanso kugwirisa ntchito malingaliro anu abwino! Zambiri za izi pa Chaputala 20.)

MOMWE MULUNGU AMAONERA MATENDA

Ngati mumvetsetsa mmene Mulungu amaonera nthenda simudzakhala ndichikayiko komwe ichokera. Mulungu amayitcha nthenda ukapolo

Ndipo Yehova anacotsa ukapolo wa Yobu. (Yobu 42:10)

Yesu anabwera kudzalalikira mamasulidwe ku ukapolo

Mzimu wa Ambuye uli paine, Cifukwa cace iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Anandituma Ine kulalikira am'nsinga mamasulidwe, Ndi akhungu kuti apenyenso, Kuturutsa ndi ufuru ophwanyika. (Luka 4:18)

Yesu amayitcha nthenda kumangidwa

Ndipo mkazi uyu, ndiye mwana wa Abrahamu, amene Satana anammanga, onani, zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu, nanga si kuyenera kodi, kuti amasulidwe nsinga yace imeneyi tsiku la Sabata? (Luka 13:16)

Yesu anabwera kudzamasula amsinga ndi choonadi

Nndipo mudzazindikira coonadi, ndipo coonadi cidzakumasulani. (Yohane 8:32)

Yesu amaona nthenda ngati kuponderezedwa ndipo anachiritsa iwo akuponderezedwa:

Ndipo anamuza kuti aimitse gareta; ndipo anatsikira onse awiri kumadzi, Filipo ndi mdindoyo; ndipoanambatiza iye. (Machitidwe 10:38)

Baibulo nthenda ndi imfa ndi adani:

Mdani wotsiriza amene adzathedwa ndiye imfa. (1 Akorinto 15:26)

Nthenda imatchedwa zonyasa:

Pakuti m'cuuno mwanga mutentha kwambiri; Palibe pamoyo m'mnofu mwanga. (Masalmo 38:7)

Nthenda imaonedwa ngati Choipa:

Camgwera cinthu coopsa, ati; Popeza ali gonire sadzaukanso. (Masalimo 41:8)

Pali mavesi mu Baibulo omwe amaonetsa kuti Mulungi anatuma mirili ndi matenda. Pamene mulungu si gwero alazinthu zoipazi pa dziko, nthawi zina amazigwiritsa ntchito ndicholinga chokakwaniritsa chifuniro chake chopereka chiweruza kwa mdani.

CHIPULUMUTSO KU TEMBERERO

Mwaphunzira mu phunzirori kuti matenda ndi imfa ndi mbali ya temberero la tchimo, koma Agalatiya 3:13 akuti, “Yesu anatiomnola ife kuchokera ku temberero la chilamulo.” Pamene Yesu anafa pa mtanda, anatenga temberero la tchimo ndi imfa pa iye mwini ndipo...

...monga mwa kulakwa kumodzi (Adamu) kutsutsa kunafikira anthu onse; comweconso mwa cilungamitso cimodzi (Yesu Khristu) cilungamo ca moyo cinafikira anthu onse.

Pakuti monga ndi kusamvera kwa munthu mmodzi ambiri anayesedwa ocimwa, comweco ndi kumvera kwa mmodzi ambiri adzayesedwa olungama. (Aroma 5:18-19)

Chipulumutso ndi machilitso ndi phindu ya nsembe yimene Yesu anapereka pa mtanda wa Kavale. Kudzera mwa imfa yake ndi kuuka kwake, Yesu anatenga temberero ya tchimo, matenda ndi imfa mmalo mwanu. Chifukwa anapereka dipo la tchimo, inu simukeyenera kuti mupereke. Chifukwa anatenga nthenda zanu, simukuyenera kuti mupereke, Chifukwa anauka mu kuuka kwa akufa, inu muzauka! Satana amabwera kuzapha, kuba, ndikuononga, koma Yesu anati...

...ndadza Ine kuti akhale ndi moyo, ndi kukhala nao wocuruka. (Yohane 10:10)

Mukalandira Yesu ngati Mpulumutsi, temberero la tchimo limasweka. Nngakhale mumakhala mu thupi la dothi yomwe imaperekedwa ku kulimbana ndi ntchimo ndi matenda, inu siothedwa ndi temberero. Yesu wakuombolani kuchokera ku temberero la chilamulo! Pamene mukufunsa gwero la matenda (kapena chinachirichonse) chomwe chimabwera mu moyo wanu, muzifunse nokha, “kodi chimapha, kuba, ndikuononga?” Ngati ziri chomwecho, Satana ndi gwero. “Kodi chikundipangisa kuti ndikhale ndi moyo wochulukuka?” Ngati ziri choncho, gwero lake ndi Mulungu. Kumbukiraninso kuti...

Mphatso iri yonse yabwino, ndi chininkho ciri conse cangwiro zicokera Kumwamba, zotsika kwa Atate wa mauniko, amene alibe cisanduliko, kapena mthunzi wa citembenukiro. (Yakobo 1:17)

Zifunsemi nokha: “Kodi mabvutowa ndi mphatso yambwino ndi chininkho?” Koma ngati simungayankhe kuti “eya,” ndipo muvomereze kuti Mawu amati: Matenda sachokera kwa Mulungu!

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Kodi matenda ndi imfa zinalowera bwanji mu dziko?

3. Kodi gwero la matenda ndi ndani?

4. Kodi Mulungu amaona bwanji matenda?

5. Kodi mwaphunzira chani muphunzirori zokhuza zinthu zowononga za matenda?

6. Kodi mungamasuke bwanji temberero la matenda ndi imfa.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Ngati mungabweretse malingarilo ano mogwirizana ndi malngaliro a Mulungu, kodi matenda mungawaone bwanji?
-

2. Mulungu si gwero la mabvuto koma atha kuwagwiritsa ntchito ndicholinga chofuna kukaniritsa zolinga zake. Werengazi zitsanzo zotsatirazi zomwe zikuonetsa izi:

-Miririi ku Igipto:	Eskodo 7-11
-Khate la Miliyamu:	Numeri 12:10
-Matenda a Mfmu Yeholamu:	2 Mbiri 21:18
-Khate la Gehazi:	2 Mafumu 5:27
-Imfa ya mwana wa Davide:	2 Samueli 12:18
-Imfa ya ana a Eli:	1 Samueli 2:34
-Mabvuto a Yobu:	Buku la Yobu
-kubvutika kwa Yosefe	Genesis 45:5-7
-Kupachikidwa kwa Yesu	Marko 14:35-36 ndi Aroma 5:6-12
-Kumangidwa ka Paulo	Afilipi 1:12,19
-Minga mu thupi la Paulo	2 Akorinto 12:7

3. Ganizirani nyengo zimene munakumana nd mabvuto. Kodi Mulungu anazigwiritsa bwanji ntchito ku ulemerele wake?
-

4. Mulungu si gwero la mabvuto anu, kodi mukuganiza kuti angazigwiritse bwnji nchito ku ulemerele wake? Pemphererani izi.
-

5. Kodi mwaphunzira chani muphunzirori zomwe mungagwiritse ntchito kulimbikitsa amene akubvutika? Gawanani nawo musanapitirire ku phunziro lina
-

6. Zifunsemi nokha mafunso otsatirawa za matenda anu apena amene mukumutumikira:

-kodi chimapha, kuba, ndikuononga? Ngati ziri chomwecho, Satana ndi gwero. (Yohane 10:10)

- Kodi chikundipangisa kuti ndikhale ndi moyo wochuluka? Ngati ziri choncho, gwero lake ndi Mulungu. (Yohane 10:10)

-Kodi ndi mpatso yambwino ndi chininkho? Ngati ayi, ndiye kuti sizikuchokera kwa Mulungu (Yakobo 1:17)

7. Kodi mukukhulupirira kuti mwawomboledwa kut temberero la imfa ndi matenda? Ngati ayi, onaninso Chaputala ichi kachikena.

CHAPUTALA 5

ZIFUKWA ZA MATENDA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kuzindikira zifukwa zisanu za matenda
- Kufotokoza momwe matenda ali chotsatira cha kuphwanya malamulo auzimu.
- Kufotokoza momwe matenda ali chotsatira cha zichitochito za Satana.
- Kufotokoza momwe matenda ali chotsatira cha kuphwanya malamulo a Mulungu.
- Kufotokoza momwe kuzindikira kosayenera Thupi la Khristu kumabweretsa matenda.
- Kufotokoza malangizo a m'Baibulo oyitana kuwononga thupi kuti mzimu ukapulumuke.

LONJEZO LA MACHIRITSO

Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Sindidzaiwala malangizo anu nthawi zonse; Popeza munandipatsa nao moyo. (Masalmo 119:67,71,93)

CHIYAMBI

Pali gwero limodzi la matenda ndiye Satana, koma pali zifukwa zosiyanasiyana zimene matenda amabwerera pa inu. Nazi zifukwa zina za matenda:

KUPHWANYA MALAMULO AUZIMU:

Pamene munthu anachimwa, imfa inayamba kugwira ntchito yachinyengo mthupi:

Chifukwa chakenso, pamene munthu wachimwa nalowa m'dziko, imfa ndi tchimo; ndipo imfa inadutsa pamunthu aliyense, pakuti onse anachimwa. (Aroma 5:13).

Pakuti mphoto yake ya uchimo ndi imfa. (Aroma 6:23)

Kudwala kwa munthu sichifukwa chamachimo a iwo okha ayi, komabe yesu ananena momveka bwino muchitsanzo cha munthu osaona chibadwire (Yohane 9:1-3). Chikhala kuti Mulungu amapereka chilango chatchimo ndi matenda, bwenzi ochimwa aliyense kapena mkristu aliyense yemwe wachimwa m'dziko atadwala. Ndizoona kut tchimo ndi matenda ndizolumikizana, koma tikuyenera kusamala ndimmene zinthuzi mmene zili zolumikizidwira kwa munthu. Ikhoza kugwiritsidwa ntchito ngat njira yabwino yokanira matenda ndi zifukwa zamphamvu zathu za ife tokha.

China mwa zinthu zolakwika zomwe timagwiritsa ntchito malemba molakwika ndikut matenda amabwera chifukwa chakuchimwa kwa munthu kapena kusowa chikhulupiliro. (limene lili tchimo).

Ngati waphwanya lamulo la Mulungu, mudzavutika, kuzunzika uku ndikwamchitidwe wa uchimo wa inu nokha. Pakuti ndicho chiweruzo cha wochimwa. Kwa okhulupilira, ndichilango. Mwachitsanzo okhulupilira yemwe akuzipezeketsa mukusakhulupirika akhoza kupeza nazo chilango (monga nthenda ya edzi) monga osakhulupilira aчитira. Ngakhale musunga lamulo la Mulungu, mukhozabe kuzunzika chifukwa mukukhala m'dziko lodzadza ndi uchimo. Nthawi zina chilungamo chimasowa chifukwa tikukhala m'dziko la uchimo. Chitsanzo chakuzunzika ndi tchimo lako lomwe ndi ngati munthu otenga edzi kudzera mchikhalidwe chake choipa. Chitsanzo cha kuzunzika chifukwa chakupezeka kwa tchimo m'dziko ndi wina kutenga matenda a edzi pamene akulandira magazi kuchipatala.

Mabaibulo ambiri akutsimikiza kuti matenda akhoza kulingana uchimo wa munthu (mariko 2:1-12; Yohane 5:1-11,14; yakobo 5:14-16; masalimo 38:3,7). Aroma 6:19 akutsimikiza kuti zonyansa zonse zimabwera chifukwa cha uchimo. Pamene tayang'anira mzimu wa chilamulo, timayenda muthembelerolomwe linafotokozedwa ku Deteronomiyo 28. Matenda akhoza kulingana ndi tchimo la mgwirizano (machitidwe 5:1-11; 1 akorinto 11:27-32).

Machiritso akhoza kutayika chifukwa chobwereranso ku tchimo:

Zitapita izi Yesu anampeza m'Kachisi, nati kwa iye, Taona, wachiritsidwa; usachimwense, kuti chingakugwere choipa choopsa. (Yohane 5:14)

KUPHWANYA MALAMULO A CHILENGEDWE CHA MULUNGU:

Matenda ena amabwera pa ife anthu chifukwa tinaphwanya malamulo achilengedwe cha Mulungu. Mwachitsanzo:

- Kudya kosayenera.
- Kugwira nchito mopyola muyeso, kupanga zinthu mwaphuma.
- kupumula kosakwamira.
- kusadziletsa komwe kumabweretsa mkwiyo, kuwawidwa mtima ndi zina zotero.
- kusowekera ubale wabwino ndi anthu ena (kuwawidwa mtima, kusakhululuka).
- masewera olimbitsa thupi (kuchulutsa kapena kuchepetsa).
- kumwa mankhwala ozunguza bongo komanso kumwa mowa mwa uchidakwa. Kuyika zinthu za poyizoni mthupi.
- kumphwanya chilengedwe cha lamulo monga ngati lamulo loti chilichonse chokwera mmwamba chitsike pansu.
- Mwadaladala kuzipezeketsa muchiopsezo kudzera mumachita chita angozi komanso kukana kugwiritsa ntchito zida zodzitetzera (monga kumanga lamba pampano wamugalimoto, kuvala magalasi pomwe munthu ukugwira ntchito, chipewa chozitetzera pomwe ukugwira ntchito ya zomangamanga).

ZIWEMBU ZA SATANA:

Thenda yobwera chifukwa cha tchimo chiyambi chake chaimakhala mwa satana. Yobu ndi chitsanzo chimodzi cha zimezi (onani Yobu 1 ndi 2). Yobo anakumana ndi matenda chifukwa chachiwembu cha Satana. Samabvutika chifukwa cha tchimo la iye. Umboni wa Mulungu okhuza Yobu unali wakuti anali munthu wachiyero.

Tchimo ndi chiwembu chokonzedwa ndi satana pa munthu wa uzimu. Thenda ndi chiwembu chake pa munthu kuthupi. Mu Chipanano Chatsopano, ngakhalenso mu nyengo yatsopano, olungama amavutika kwambiri ndiziwembu za satana chifukwa choti tili pankhondo ndi satana, ndipo munkhondo iliyonse pamakhala ngozi.

Satana amapangira chiwembu thupi lanu monganso achitira ndi malingaliro anu. Malingaliro anu, thupi, ndi munthu wakale (chilakolako chamaso, thupi ndi kuzikuza mmoyo), ndinjira zomwe amapangira ziwembu. Ngakhale achita chiwembu kuthupi chomwechonso ku uzimu, alibenso ufulu okhala mmoyo wanu wakuthupi koma kukhala kumoyo wanu wa uzimu.

Machitidwe amphamvu asatana kuthupi la okhulupilira akhoza kulinganizidwa ndi nkondo ya gerila. Ndipo alibe ufulu weniweni mmadera monse koma amafuna kumangochita mulimonse.

KUSAZINDIKIRA KWENIKWENI THUPI LA KHRISTU:

Paulo anati ambiri anali ofooka ndi odwala chifukwa sanazindikira bwino Thupi la Khristu ndi kutenga mgonero osafunikira. Mgonero ndikutenga mkate ndi vinyo zomwe zimaimirira thupi ndi mwazi wa Yesu Khristu. Paulo anachenjeza

Cifukwa cace yense amene akadyamkate, kapena akamwera cikho ca Ambuye kosayenera, adzakhala wocimwira thupi ndi mwazi wa Ambuye.

Koma munthu adziyese yekha, ndi kotero adye mkate, ndi kumwera cikho.

Pakuti iye wakudya ndi wakumwa, adya namwa ciweruziro kwa iye yekha, ngati sazindikira thupilo.

Cifukwa cace ambiri mwa inu afoka, nadwala, ndipo ambiri agona. (Akorinto 11:27-30)

Mutha osazindikira Thupi la Khristu mu njira zitatu:

TANTHAUZO LA MWAZI NDI THUPI:

Mumalephera kuzindikira Thupi la Khristu ngati simumvetsetsa tanthauzo la chipatso cha vinyo ndi mkate. Zinthu zakuthupizi ndi chizindikiro ya uzimu cha mazi ndi thupi la Yesu. Ingakhale anthu ambiri amamvetsetsa kuti mwazi wa Yesu umatsuka machimo, nthawi zambiri sazindikira tanthauzo lenileni la Thupi la Khristu. Thupi la Khristu linasweka chifukwa cha machilitso anu (onani Yohane 6:48-58 ndi Luka 6:48-51).

KUGAWANIKANA MU THUPI:

Nthawi zina timalephera kuzindikira Thupi la Khristu pakusazindikira kulumikizana kwenikweni komwe tiri nako ndi abale ndi alongo mwa Ambuye. Kugawanikana kukachitika mu mpingo, ife sitikuzindikira bwino Thupi la Khristu. Timadya ndi kumwa kosayenera ngati sitikumvetsetsa ubale wathu wa uzimu ndi abale ndi alongo mwa Ambuye. Paulo anafotokoza pa 1 Akorinto 3:1-13 kuti Akhristu akuthupi okhuziidwa mukugawana sangatenge gawo mu Mawu chifukwa cha umunthu wawo.

KUDYA KOSAYENERA:

Timadya mosayenera pamene tikutenga mgonero ndi moyo usawunikiridwa. Zifooko ndi madwale amachokera pakuchita izi. Ndichifukwa chake Paulo anati tikuyenera kuziona tokha mu uzimu ndi kulapa tisanayambe kutenga mgonero.

CHIONONGEKO CHA THUPI KUTI MZIMU UPULUMUTSIDWE

Mulungu amalolera anthu ena kwa satana kuti akaonongedwe ndicholinga choti akalandire mwambo. Mulungu samapereka matenda pa iwo, koma amalolera kuti zichitike ndithu. Mukhoza kuwerenga pa 1 Akorinto 5:1-7. Baibulo likunena:

Kodi zingachitike bwanji: zimachitika pa...

- Umodzi.
- Mu uzimu ndi mphamvu ya ambuye.
- Mudzina la Ambuye.

Nchifukwa chani zimachitidwa: Zimachitika chifukwa...

- chiwerewere.
- halidwe loipa kuposa ladziko.
- kudzikuza.
- Kusowekera kulapa.
- Uchimo pakati pa anthu aMulungu.

Cholinga chake: Munthu: chionongeko chathupi ndicholinga kuti mzimu ukapulimutsidwe.
Machitidwe: Kuchotsa choipa mwachangu chisanaononge ena.

MAYESO OZOYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Kodi zifukwa zisanu za matenda ndi ziti?

3. Kodi matenda ali bwanji chotsatira cha kuphwanya malamulo auzimu?

4. Kodi matenda ali bwanji chotsatira cha zichitochito za Satana?

5. Kodi matenda ali bwanji chotsatira cha kuphwanya malamulo a Mulungu?

6. Kodi kuzindikira kosayenera Thupi la Khristu kumabweretsa bwanji matenda?

7. Fotokozani malangizo a m'Baibulo oyitana kuwononga thupi kuti mzimu ukapululumuke.

Kodi zingachitike bwanji? _____

Nchifukwa chani zimachitidwa? _____

Cholinga chake? _____

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Ganizirana chifukwa chimene mukudwalira kapena amene mukumutumikira. Kodi ndi...
 - Kuphwanya malamulo auzimu?
 - Kuphwanya malamulo a chilengedwe cha mulungu?
 - Ziwembu za satana?
 - Kusazindikira kwenikweni thupi la khristu?
 - Chionongeko cha thupi kuti mzimu upulumutsidwe?

2. Mukuganiza kuti inu muli (kapena munali) odala chifukwa chakulangidwa? Kodi mupage chani (kapena munapanga chani) kutengera pa Yakobo 5:14-16?

3. Ngati nthedwa yanu kapena iye amene mukumutumikira ndi chifukwa chophwanya malamulo a chilengedwe cha Mulungu, kodi mungapanga chani kuti mukonze izi?

4. Ngati nthedwa yanu kapena iye amene mukumutumikira ndi chifukwa chophwanya malamulo auzimu a Mulungu, vomerezani ndi kulapa tchimo lani ndi kufunsa 1 Yohane 1:8-9, kapena atsogozeni kuti apange chomwecho.

5. Kodi mukuganiza kuti inu kapena munthu amene mukumutumira sanazindikire bwino Thupi la Khristu? Ngati ziri choncho, lapani, ndi kupempha chikhulupiriro, ndipo apemphereni kuti achiritsidwe.

6. Ngati mukuganiza kuti matenda anu kapena a munthu amene mukumutumira ayamba chifukwa cha chiwembu cha ziwana, mmangani mzimu wachifooko mu pemphero ndi kumasula mphamvu ya machiritso ya Mzimu Woyera

7. Werengani lonjezo la machiritso

Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Sindidzaiwala malangizo anu nthawi zonse; Popeza munandipatsa nao moyo. (Masalmo 119:67,71,93)

Ndimeyi ikubvumbulutsa Davide anakumana ndi mabvuto chifukwa cha kuphwanya malamulo auzimu. Kodi anaphunzira chani muzokumana zake? Kodi ndi chani chinabweretsa machiritso ku nyengo zake? Kodi mungagwiritse ntchito bwanji zomwe Davide anaphunzira mu moyo wanu?

CHAPUTALA 6

MITUNDU YA MATENDA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kulemba mitundu isanu ya matenda.
- Kufotokoza kudwala kwa uzimu
- Kufotokoza kudwala kwa kuthupi
- Kufotokoza kudwala kwa maganizo
- Kufotokoza kudwala kwa misala
- Kufotokoza matenda a ziwanda

LONJEZO LA MACHIRITSO

Mundicitire cifundo, Yehova; pakuti ndalefuka ine: Mundicize, Yehova; pakuti anthunthumira mafupa anga. Moyo wanganso wanthunthumira kwakukuru; Ndipo Inu, Yehova, kufikira liti? Wamva Yehova kupemba kwanga; Yehova adzalandira pemphero langa. (Masalmo 6:2-3,9)

CHIYAMBA

Pamene tikuyakhula za kudwala kapena matenda timatanthauza chikhalidwe chomwe chiri chosagwirizana ndi ndi mmene ziriri kunmwamba mmene Mulungu analengera. Pali magulu asanu amatenda:

KUDWALA KWA UZIMU:

Kudwala kwa uzimu ndi tchimo. Ngati sithana nalo, ndi dula moyo wauzimu. Machiritso a thenda ya uzimu ndi kukhululukidwa kwa tchimo kupyolera mwa Yesu Khristu. Ndi machiritso opambana kuposa onse, monga ngati kuti ukadaulo wamakhwala ndi machiritso auzimu sangathe kuchita kanthu pamadwale awa.

KUDWALA KWAKUTHUPI:

Kudwala kukhoza kubwera chifukwa chakusokonekera kwa thupi. Ndi mavuto oti akhoza kuzindikiridwa ndikuwonedwa ndi akatswiri achipatala. Kudwala kwa thupi kutha kubweranso chifukwa chakusokonera kapena kusagwira bwino kwa ziwalo zathupi. Awa ndi matenda amene amabwera chifukwa chakusokonekera kwa chiwalo chimodzi zomwe zimapangitsa kuti thupi lonse lisokonekere. Matenda odziwika bwino ndi monga matenda a mtima, kuthamanga kwa magazi, shuga, tizilonda tammimba ndi ena otero. Ngati matenda akhalitsa osachizidwa amatha kuwononga ziwalo zina. Chifukwa chakugwirizana kwa thupi la munthu, kudwala kwa mbali imodzi kukhoza kunkhudza thupi lonse.

KUBWALA KWA MAGANIZO:

Kudwala kwa maganizo kumabwera chifukwa chamaganizo oipa monga ngati mkwiyo, kuwawidwa mtima, ndi zina zotero. Kuti izi zichiritsidwe Mulungu akuyenera kukhudza maganizo amkati. Ena amawatchula kuti “machiritso amkati,” ngakhale mauwa nthawi zina amagwiritsidwa ntchito molakwika ndipo amakuzidwa mkumatanthauza zomwe Baibulo silimaphunzitsa.

KUDWALA MISALA:

Matenda amasila amayamba chifukwa chakudwalitsa nthawi yayitali, kukhumudwa, zilema zobadwa nazo ndi zina zomwe sizimabwera ndi satana.

MATENDA A ZIWANDA

Mwamatenda ena amene amabwera chifukwa cha ziwanda ndi monga kugwidwa ndi mizimu yoyipa, kuponderezedwa, komaso ziwanda zina zimachititsa munthu kudwala matenda amasila ndi matenda ena akuthupi. Matenda obwera ndiziwandawa amafuna machiritso ake apaderadera omwe amatchulidwa kuti mamasulidwe. Mamasulidwe ndi machiritso ndi ofanana, koma malemba amawasiyanitsa:

Ndipo Iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda.

**Ndipo anawatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu ndi kuchiritsa anthu odwala.
(Luka 9:1-2)**

Muphuznira zambiri zokhuza matenda a ziwanda mu Gawo la chinanu ndi chimodzi la phunzirori.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Kodi mitundu isanu ya matenda ndi chani?

3. Kodi kudwala kwa uzimu ndi chani?

4. Kodi kudwala kwa kuthupi ndi chani?

5. Kodi kudwala kwa maganizo ndi chani?

6. Kodi kudwala kwa misala ndi chani?

7. Kodi matenda a ziwanda ndi chani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Ndipemphero santhulani matenda anu kapena a munthu yemwe mukumutumiira. Kodi ndi mtundu wanji wamatenda omwe mukuthana nawo? Kodi ndi...

- ___ Kudwala kwa uzimu?
- ___ Kudwala kwakuthupi?
- ___ Kubwala kwa maganizo?
- ___ Kudwala misala?

2. Lembani phunziro chifukwa chimene mukuganiza kuti ndi...

Kudwala kwa uzimu:

Kudwala kwakuthupi:

Kubwala kwa maganizo:

Kudwala misala

3. Chifukwa cha chikhalidwe cha uchimo, matenda ali mbali imodzi ya thupi la munthu. Kodi mukuona kuti izi ndizoona mu moyo wanu kapena wa iye amene mukumutumikira?

Kodi kudwala kwa kuthupi kumakhuza bwanji mzimu, maganizo ndi maganizo?

Kodi matenda a uzimu amakhuza bwanji thupi, maganizo ndi maganizo?

Kodi matenda a maganizo (maganizo) amakhuza bwanji thupi, maganizo ndi mzimu?

Kodi matenda a misala amakhuza bwanji thupi, mzimu ndi maganizo?

4. Werengani mavesi amachiritso a phunzirori omwe akupezeka pa Masalimo 6:

Mundicitire cifundo, Yehova; pakuti ndalefuka ine: Mundicize, Yehova; pakuti anthunthumira mafupa anga (vesi 2). Moyo wanganso wanthunthumira kwakukuru; Ndipo Inu, Yehova, kufikira liti? (vesi 3). Wamva Yehova kupemba kwanga; Yehova adzalandira pemphero langa (vesi 9).

Vesi 2 ikuonetsa matenda akuthupi: “pakuti anthunthumira mafupa anga.” **Vesi 3** ikuonetsa matenda auzimu: “Moyo wanganso wanthunthumira.” **Vesi 3** ikuonetsa kuti Olemba anadikirira machiritso: “Ndipo Inu, Yehova, kufikira liti?” (Kodi inu munafunsapo funso iri pokhuzana ndi machiritso?) **Vesi 9** ikuonetsera chikhulupiriro chake mwa Mulungu: “Wamva Yehova kupemba kwanga” (“wamva” mnene wakale). “Yehova adzalandira pemphero langa” (“adzalandira” mneni watsogolo). Pemphero lake lamachiritso lamveka, ingakhale mayankho ake azaonekera mtsogolo.

CHAPUTALA 7

ZOTSATIRA ZA MATENDA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kuzindikira mathero awiri amatenda
- Kuzindikira mitundu iwiri ya imfa.

LONJEZO LA MACHIRITSO

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero. (Yeremiya 29:11)

CHIYAMBI

Pali mitundu iwiri ya zotsatira za matenda. Zitha kukhala ku ulemerero wa Mulungu kapena matenda aku imfa.

Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero. (Yeremiya 29:11)

CHIFUKWA CHA ULEMELERO WA MULUNGU

Matenda otengera ulemerelo wa Mulungu ndi amene munthu amalemekeza Mulungu mu umboni, moyo ndi utumiki. Mutha kuwerenga nkhani ya munthu amene anali osaona chibadwire pa Yohane 9. Yesu anati zokhuzana ndi kusaona kwa munthuyu:

...Sanachimwa ameneyo, kapena makolo ake, koma kuti nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa iye. (Yohane 9:3)

Pamene munthu wosaona anachiritsidwa, Mulungu analandira ulemerero kudzera mu umboni wake. Mulungu nthawi zonse azilandira ulemerero. (tikamati “zovomerezeka” tikuthanthauza kuti machiritso osapembedza Satana)

MACHIRITSO ACHIRENGEDWE:

Mulungu nthawi zambiri amalandira matamando pa machiritso aumulungu, koma, ulemereronso ukuyenerera kupita kwa Iye pa zomwe tikuti machiritso achirengedwe. Mulungu analenga thupi ndikuonetsera chikhalidwe chake ndi mphamvu yake yolenga kudzera mukachitidwe ka chirengedwe mu thupi la munthu.

MACHIRITSO A KUCHIPATALA:

Matamando akuyenera kupitanso kwa Mulungu pa machiritso omwe athandidzidwa ndi kuchipatala. Baibulo limati mphatso inailiyonse yabwino imachokera kwa Mulungu (Yakobo 1:17) ndipo izi zimaphatikidza makhwala, zakudya zamavitamini, ndi zinthu zina zomwe zimathangatira zithupi lanu. Mankhwala ambiri amachokera ku kudzakudya za mitengo ndi zinthu zomwe zinalengedwa ndi Mulungu.

POMPOPOMPO NDI KUCHEDWETSA

Nthawi zina munthu amatha kuchiritsidwa pompopompo, koma nthawi zina machiritso amachedwa ndikuti munthu akhoza kudzachiritsidwa pambuyo pake kapena pang'onopang'ono. Zitsanzo:

-Zakaria sanachiritsidwe mpaka kubadwa kwa Yohane: Luka 1:20

-Hanna sanabereke mwana kufikira nthawi yoyikika ya Mulungu: 1 Sammueli 1:5-19

- Abraham ndi sara sanabereka mwana kupatula kuti Abrahamu anali wachikhulupiliro, kufikira nthawi yoyikika ya Mulungu;(Aheberi 11:11)

MATENDA OKUTENGERA KU IMFA:

Ku Yohane 11:4 Yesu anati nthenda ya Lazaro sinali yomutengera ku imfa. Zomwe zikuthanthauza kut pali nthenda zokutengera ku imfa. Pali mitundu iwiri ya imfa yomwe baibulo limafotokoza. Ena omwe amene aperekedwa kuchiwonongeko cha chathupi amamwalalira mwansanga ndicholinga chakuti mzimu wawo ukhoza kukapuluma.

Munthu aliyense ali ndi nthawi yoyikika yoti amfe (Mlaliki 3:2; Ahebri 9:2). Ngakale Elisa, mneneri wamphamvu wa Mulungu anachita zozizwa zambiri zamachiritso, anadwala “nthenda ija adafa nayo” (2 Mafumu 13:14). Ndizotheka kungoleka kupuma osadwala:

...mukalanda mpweya wao, zikufa, nizibwerera kupfumbi kwao. (Salimo 104:29b)

Mose monga ngati munthu wokalamaba analibe zovuta za kukula kwake. Yoswa anali “wokalamba”. Mulungu amasunga ena mwauzimu, pamene ena akukumana ndi zovuta chifukwa cha ukamba. Mulungu amatisunga kaya matupi anthu akutsata njira yachilengedwe yokalambira ndi kumwalira ndi matenda kapena akutetezedwa ndi mphamvu ya kumwamba. Cholinga chamachilitso sikuti mkusamwalira. Machiritso akumwamba safikira zomwe zirizonse zimene makhwala amachita. Ngakhale onse amene anaukitsidwa ndi Yesu kwa akufa mapeto ake anazafanso.

Pamene okhulupilira wamwalira, ndimachiritso amphumphu kumoyo osatha. Timalakwitsa pakukhala ndimoyo wozipatsa malire ndi nthawi mmalo mokhala mmoyo osatha. Ngati okhulupilira, tikukhala mmoyo wosatha ngakhale pomwe tili amoyo mmoyo uno ingakhalenso pomwe tamwalira.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Kodi mathero awiri amatenda chani?

3. Kodi mitundu iwiri ya imfa ndi ili?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Ngati matenda anu kapena amunthu yemwe mukumutumikira ndiosachiritsika, ndi Mulungu yekha amene angaulure kuti ngati ali “matenda aku imfa” kapena aku “ulemerero wa Mulungu.” Pokhapokha Mulungu ataulula kuti ndi aku imfa, pitirizani kupempherala machiritso monga mwa chifuniro cha Mulungu.
2. Machiritso akuchipatala ndi achiregedwe amachokera kwa Mulungu, monga aliri machiritso aumulungu. Bvuto limakhalapo ngati anthu atama mankhwala kapena madokotala malo mozindikira kuti Mulungu ndi gwero la machiritso onse. Yesu anati kwa Israyeli:

koma sanadziwa kuti ndinawaciritsa. (Hoseya 11:3)

Mfumu Asa anamwalira chifukwa anafuna chithandizo chakuchipatala chokha. Ananyalanyaza chikhalidwe chazimu ndipo sanabwerere kwa Ambuye mu nyengo zakusowa (2 Mbiri 16:12)

3. Kodi mungakumbukire matendo omwe mukadwala omwe machiritso ake anachtika chifukwa cha kugwiritsa ntchito mankhwala, madotolo, kapena chilengedwe cha thupi?
_____ Kodi munathokodza Mulungu chifukwa chamachiritsowo?
_____ Ngat ayi, chitani chomwecho.
4. Pomwe inu kapena munthu yemwe mukumutumikira wachiritsidwa, kodi mugwiritsa ntchito bwanji machiritsowa kulemekedza nawo Mulungu?

5. Ngati matenda anu ali aku imfa pomwe nthawi yanu yakufu ku thupi yakwana, kumbukirani kuti inu mukukhalabe ndi moyo wosatha. Muchiritsidwa. Mulowa mu kupezeka kwa Mulungu ndi thupi langwiwo!

GAWO LACHITATU

KUBWEZERA CHIWEMBU

Mu gawo langothali mwaphunzira chiwembu cha woyipayo pa matupi pamene mumaphunzira gwero, zifukwa, mitundu, ndi zotsatira za matenda.

Mu gawo lino muphunzira momwe mungabwezere chiwembu kwa Satana. Kubwezera chiwembu ndi kumenya nkhondo ndicholinga kugonjetsa chiwembu cha woyipayo.

Kuti mubwezere chiwembu cha Satana pa matupi anu mukuyenera kumvetsetsa

- MAZIKO AMACHIRITSO A M'BAIBULO
- ZOLINGA ZA MACHIRITSO
- MPHATSO ZA MACHIRITSO

Iyi ndi mitu ya gawoli.

CHAPUTALA 8

MAZIKO AMACHIRITSO A M'BAIBULO

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kufotokoza fanizo lamu Chipangano Chatsopano la wofesa mene limakhuzanirana ndi machiritso.
- Kulemba mwachidule ziphunzitso za Muchipangano Chakale za machiritso.
- Kugwiritsa ntchito zitsanzo za Yesu ndi Mpingo woyamba, polemba mwachidule ziphunzitso za machiritso amu Chipangano Chatsopano.
- Kuzindikira machiritso ngati phindu la nsembe ya Yesu Khristu.
- Kulemba mwachidule Utumiki Waukulu poyerekezera ndi machiritso ndi mamasulidwe.
- Kulemba zitsanzo za m'Baibulo zomwe zimatsimikidza kuti okhulupirira onse azitengapo ngawo pa machiritso ndi mamasulidwe.
- Kudzindikira mafungulo itatu ya Ufumu yomwe imakhuzana ndi machiritso.

LONJEZO LA MACHIRITSO:

Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natundudwidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. (Yesaya 53:5)

CHIYAMBI

Ndi phunziro iri muyamba ulendo wa chikhulupiriro mu machiritso ndi mamasulidwe. Baibulo ndiro chitupa chanu chapaulendo. Mu dziko lakuthupi, chitupa chimatsimikiza kuti ndinu mnzika ndi kutsimikiza mwayi umene dziko limapereka.

Ngati chitupa chazimu, Mawu a Mulungu amatsimikidza unzika wanu mu Ufumu wa Mulungu. Amatsimikiza kuti ngati okhulupirira obadwanso mwatsopano ndinu oyenera kulandira zonse zomwe unzikawu umapereka, kuphatikiza mwayi okhala ndi machiritso ndi mamasulidwe aumulungu.

MAWU A MULUNGU NDI MACHIRITSO

Muwerenge fanizo lawofesa pa Mateyu 13:3-8, 18-23; Marko 4:3-8, 14-20; ndi Luka 8:5-8, 10-15. Mu fanizo iri, Yesu akufotokoza kuti “mbeu” ndi Mawu a Mulungu. Mu dziko lakuthupi mbeu iri ndikuthekerera mwa iyo kubweretsa moyo, koma iribe mphamvu ngati sibzalidwa ndi kutsamalira.

Chomwecho ndi choona mu dziko la uzimu. Mbeu ya Mau a Mulungu iri ndi kuthekera kobweretsa moyo wa uzimu. Mbeu ya Mawu a Mulungu ya machiritso iri ndi kuthekera kobwerensa mamasulidwe. Koma pokhapokha mbeu ya Mawu yabzalidza mu moyo wanu, inu muziyesera kukolola musanabzale. Simungakolole pomwe simunabzale. Ich ndichifukwa mukuyenera kuphunzira maziko a m’Baibulo amachiritso. Lamulo limodzi lakukolola ndilakutu kuti mukolole, mukuyenera kubzala.

Lamulol lina lakukolola ndilakuti simukolola nyengo yimene mwafesa mbeu, koma mumakolola munyengo yake yoyikika. Pamene mukuyamba kubzala Mawu a Mulungu mu moyo mwanu, simungakumane ndi machiritso pompopompo kapena kuona zotsatira mwa iwo mukuwatumikira. Koma ngati mungapitirire kubzala Mawu amachiritso, pamapeto pake muzakolola—ndi lamulo la kukolola.

Fanizo lawofesa iritso ndi machenjezo ena omwe mukuyenera kudziwa pamene mukuyamba kuphunzira zimene Baibulo limaphzunzitsa zamachiritso. Pamene mbeu ya Mawu a Mulungu ikubzalidwa palinso kutsutsana kwa Satana.

Mbeu zina zimagwera “panjira” ya moyo wanu ndipo oyipayo amaziba kuchokera kwa inu. Mumamva Mawu a Mulungu a amchiritso ndi mamasulidwe, koma mumalolera kuti alandidwe, mwina chifukwa cha miyambo kapena kukayikira, kudzudzula, ndi kusakhulupirira.

Mbeu zina zimagwera pa “nthaka ya mwala” koma imu simumailola kuti ibazle midzu mu mtima mwanu. Nthaka ya mwala ikuyimirara mtima wouma omwe suli otseguka ku choonadii cha Mawu a Mulungu. Poyamba mau amalandiridwa ndi chimwemwe, koma mabvuto akabwera (mwina mu njira ya chiwembu cha kuthupi) kapena zotsatira za mazunzo (mwina kapena kuchokera kwa iwo omwe sakhulupirira machiritso aumulungu) Mawu amafota ndipo inu mumakhumudwa. Mbeu ya Mawu a Mulungu ithanso kutsamwidwa ndi “minga” mu moyo mwanu. Zotsamala za moyo uno, chuma, zosangalana, ndi zilakolako zimanyonga kukula kwake.

Munthu ali ndi zigawo zitatu, thupi, moyo ndi mzimu. Thupi ndi gawo la mnofu la munthu. Moyo ndi mzimu ndi zigawo za mzimu zomwe zimathekeretsa kuti munthu machitidwe, kuganiza, kumva, kuyankha mokwiya, ndi kuyankha mwa uzimu kwa Mulungu.

Zonze zimakhudzidwa pa kubzala ndi kukolola choonadi cha uzimu. kudzera mu kumva ndi kuona kwa thupi mumalandira mbeu yobala zipatso a Mawu a Mulungu. Pomwe mukumva kapena kuwerenga Mau a Mulungu amalowa mu mzimu mwanu. Koma kuti mubale zipatso mmoyo mwanu, mbeu ikuyenera kulola mu moyo wanu. Njira yake ili ngati momwe zimachitikira kuchulukitsa kwa thupi. Kutu anthu achulukane, pakuyenera kukhala mwamuna, mkazi, ndi mbeu yomwe imapatsirira pakudzela kukhalira limodzi.

Kuika izi mu uzimu, Mawu am Mulungu ndi mbeu. Mzimu ndi “mwamuna” ndipo moyo ndi “mkazi.” (tikudziwa kuti moyo ndi mbali yayikazi ya chikhalidwe cha uzimu, chifukwa Davide anati “Moyo wanga udzatamanda Yehova” pa Masalimo 34:2). Kutu tikabale zipatso, mbeu ikuyenera kulowa mu mzimu (mwamuna) ndikupatsiridwa ku moyo (mkazi).

Chifukwa chimene nthawi zambiri Mau a Muungu zamabweretsa kusntha mmoyo mwathu ndichakuti timangolora kuti alowe mumzimu mwathu basi. Sitimawalola kuti akafikire pansu pa moyo wathu.

Mu diko lakuthupi, pamene mwamuna ndi mkazi akakhala pamodzi mbeu imabzalidwa ndipo zotsatira zake zimaonekera. Moyo watsopano umabadwa ngati kamwana. Chomwechi ndizowonamu dziko la uzimu. Pamene Mawu a Malungu a machiritso akaperekedwa kuchokera ku malingaliro a maso ndi makutukupita ku mzimu ndipo amabzalidwa mu moyo wanu, zotsatira zake pamapeto pake zizaonekera mu thupi lanu.

MBIRI YA MU CHIPANGANO CHAKALE

Phunziro lathu la maziko a m’Baibulo a machiritso ndi mamasulidwe amayambira mu mbiri ya Chipangano Chakale. (Pomwe zitsanzo zosiyanasiyana zikukambidwa muphunzirori, mukhale ndi nthawi yoziwerenga mu Baibulo lanu).

Poyamba, munthu analengedwa opanda tchimo ndi wa thanzi mu thupi, moyo ndi mzimu. Mwaphunzira kale mu Chaputala 4 kuti imfa inalowa mu dziko pakutsatira tchimo la mwamuna ndi mkazi woyamba (Genesis 3). Munaphunziranso kuti pamene temberero la imfa inabwera pa munthu, Satana analowa mu thupi lamunthu ndi kuyamba kuononga ndi matenda, madwale, ukapolo, ndi imfa.

Koma mu mbiri iyi ya mdima, lonjezo loyamba lamachiritso linaperekedwa. Pa Genesis 3:15 Mulungu anati “mbeu” ya mkazi idzalalira mutu wa Satana. “Mbeu” iyi inali lonjezo la uneneri wa Yesu amene, kudzera mu utumiki wake wapadziko lapansi, imfa ndi kuukanso kwake, kudzagonjetsa Satana.

Zolembedwa zamu Genesis zimakamba za nkhani ziwiri za machiritso aumulung. Pa Genesis 17:18-19 Mulungu analonjeza kuchiritsa kusabereka kwa Sara. Pa Genesis 21:1-7 izi zinakwaniritsidwa. Genesis 20:17 ikukamba za kuchiritsidwa cha Abimereki.

Mu buku la Eskodo, matenda ndi machiritso aumulungu anayamba momveka bwino kulowa mu mbiri ya Baibulo. Pakutha kwa kupulumutsidwa kwa Israyeli kuchokera ku Igupto, anthu anayenda kwamatsiku ambiri osapedza madzi. Pamene anafika ku Mara, sanamwe madzi chifukwa anali owawa.

Mulungu anamuonetsa Mose ntengo omwe, ukaponyedwa mmadzi, upangitsa madzi kuti akhale abwino. Potsaira idzi Mulungu anadzionetsera yekha kuti ndiwochiritsa anthu ake. Anati:

...Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoono pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (1992 Eksodo 15:26)

Kutanthauzira kwabwino kwa ichi ndi “ine ndine Ambuye dokotala wanu.” Idzi zikuonetsa kakhaliidwe, kopitilira.

Chifukwa lonjezo loyambari linaperekedwa kwa Israyeli mu nyengo yoyikika, ena amati iyi imagwira ntchito kwa iwo wokha ndipo siyingagwire nchito kwa a Khristu. Koma ife tikuyenera kukumbuka, mayina a Mulungu ndi chibvumnulutsa cha chikhalidwe chake, ndipo Mulungu samasintha. Iye ngati anali dokotala ndi ochiritsa matsiko amenewo, iye alinso chimodzimodzi lero. Machiritso ena mu Eskodo ndi kuchiritsidwa kwa khate la Mose (Eskodo 4:1-7) ndi lonjezo ka Mulungu lochotsa matenda pa anthu ake (Eskodo 23:15).

Buku la Levitiko litha kuchiridwa kuti “buku la umoyo wa thanzi” la Baibulo. Mulungu anaonetsera ndondomeko zokhuzana ndi katsamaliridwe ka matenda (machitsanzo onana Levitiko 13:1-46; 14:1-32) ndi kupereka malangizo okhudzana ndi kakhaliidwe ka ukhondo (onani Levitiko 15:1-33 mwachitsanzo).

Buku la Numeri linalamba kuchiritsidwa kwa khate la Miriamu ndi Aroni (Numeri 12:1-15) ndi kuchiritsa miriri yomwe inakhudza Israyeli (Numeri 16:41-50 ndi 21:5-9).

Deutronomo 28 ndi chaputala chofunika kwambiri chokhudzana ndi machiritso. Chimakamba ubale wa kumvera ndi machiritso. Ndime zina zomwe zimatsimikiza za choonadi ichi ndi 7:15; 29:22; 30:20.

Mkazi wa Manowa anachiritsidwa kusabereka pa Oweruza 13:2-24. Muli nkhani zambiri za machiritso mu buku la 1 Mafumu. Pali nkhani za munthu ymwe anali ndi dzanja louma pa 1 Mafumu 14:4-6 ndi kuukitsa kwa mwana wakufa pa 1 Mafumu 17:17-24. Nkhani ikupitirira mu 2 Mafumu ndi kuchiritsa kwa mwana ndi Elisa pa 2 Mafumu 4:8-37 ndi kuchira kwa Namani pa 2 Mafumu 5:1-14. Muwerengetso nkhani ya Mfumu Azaria pa 2 Mafumu 15:1-12.

Kuchokera kuchiritsidwa kwa Hezekiya pa 2 Mafumu 20:1-11 timaphunzira kuti Mulungu amachiritsa matenda otsachidzika ndi kucwonjezera zaka ku moyo (onani 2 Mbiri 32:24-26 ndi Yesaya 38:1-12,16). Tikuphunziranso kuchokera ku 2 mafumu 13:14 ndi 21 kuti imfa imabwera kwa anthu onse, ngakhale kwa iwo omwe ali ndi utumiki wa machiritso.

Pembero lalikulo lakulapa lokhuzana ndi machiritso lalembidwa pa 2 Mbiri 6:26-31. 2 Mbiri 20:9 limalonjeza kuti Mulungu amamva ife tikafuulira kwa iye mu mazunzo. Pa 2 Mbiri 16 mutha kuwerenga nkhani ya Asa yemwe anafa chifukwa sanafune machiritso kwa Mulungu. Tchimo lake sirinali lopita kwa madotolo, koma kunyalanyaza Mulungu ndi mphamvu yake yamachiritso. Pa 2 Mbiri 25 mutha kuwerenga za khate la Uziya ndi pa 2 Mbiri 30:10 kuchiritsidwa kwa anthu kudzera mu pemphero la Hezekiya.

Buku la Yobu, makamaka chaputala 1 ndi 2, imatiroredza ife kudzindikira gwero la mabvuto a Yobu, kuphatikiza matenda ake. Muwerenge buku la Yobu kuti muphunzire mayankho ake mu nyengo ya matenda, momwe anawayankhira abwenzi ake, ndi momwe Mulungu anamuchiritsita ndi kumumasula iye.

Buku la Masalimo limakamba za malonjezano ochuluka, mabvumbulutso, ndi mapemphero okhuzana ndi machiritso. Werengani ndime zotsatirazi

6:2-3: “Ambuye ndichiritseni.”

27:1: “Ambuye ndi mphamvu ya moyo wanga.”

30:2: “Ndinafuula ndipo munandichiritsa.”

32:3-5: kudzindikira tchimo kumabweretsa machiritso.

34:19-20: “Masautso a wolungama mtima acuruka: Koma Yehova amlanditsa mwa onsewa.”

38:3,7: Nkwiyo ndi ntchimo zimakhuza thanzi, matenda akutchulidwa kuti “zonyasa”

41:1-8: “Chiritsani moyo wanga pakuti ime ndachimwira inu.” Matenda akutthuridwa kuti ndi oyipa.

42:11; 35:5: Mulungu ndi nkhope ya machiritso.

42:1-5: Machiritso mzimu wa khawa.

55:1-2: Pemphero lopirira ndi machiritso.

67:2: “Kuti njira yanu idziwike pa dziko lapansi, Cipulumutso canu mwa amitundu onse.”

72:13 tikuyenera kumvera chitsoni ofooka.

91:9,10: “Palibe coipa cidzakugwera, Ndipo colanga sacidzayandikiza hema wako.”

103:1-5 “Ndi kusaiwala zokoma zace zonse... Naciritsa nthenda zako zonse.” Mu ndime iyi Mulungu akuonetseredwa ngati okhululukira machimo ndi dokotala wa matenda onse.

107:17-20: “Atumiza mau ace nawaciritsa.”

119:25-28: ife timalimbikitsidwa ndi Mau.

119:67: “Ndisanazunzidwe ndinasokera.”

147:3: “Aciritsa osweka mtima.” Machiritso kwa osweka mtima.

105:37: “Ndipo anawaturutsa pamodzi... Ndi mwa mafuko ao munalibe mmodzi wokhumudwa.”

Buku la Miyambo imapereka nzeru zokhuza moyo wa thazi. Miyambo 3:7-8 ikukamba momwe tikngakhalire athanzi. Miyambo 4:2-23 ikufotokoza magwero a moyoamakhudzidwa ndi malingaliro a mtima ndi kuti Mulungu analonjeza kubweretsa machiritso.

Miyambo 15:4 ndi 30 ikutsimikiza kuti malakhulidwe abwino a amabwretsa machiritso andi Miyambi 16:24 ikuonetsa kuti Mau a Mulungu amabweretsa machiritso. Miyambo 16:24 ikuonetsa kuti Mau a Mulungu amabweretsa machiritso ku mafupa. ndipo Miyambo 17:22 ikuonetsa zotsatira za mabvuto a uzimu ku thupi.

Mlaliki 3:3 akutsimika kuti pali nthawi yoyikika ya machiritso ndipo Mlaliki 5:17 imaonetsera chisoni ndi mkiyo zimakhudzira matenda.

Yesaya 6:10 akukamba za ubale wapakati pa kumvetsetsa kwa uzimu, kutembenuka, ndi machiritso. Yesaya 19:22 akutsimikidza kuti Mulungu akachondereredwa amachiritsa (“kuchonderera” kumatanthauza “kupempha mozipereka ndi kookanikiza)

Yesaya 32:2-4 ndi unenere waukulu wa machiritso kukhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu. Yesaya 33:24 ndi 35:56 akukamba mene machiritso munthawi ya mileniamu ndi momwe okhalamo azati “ine si obwala.”

Pa Yesaya 53:5 tikulonjezedwa machiritso ndi mamasulidwe kudzera mu nsembe. Yesaya 57:18-19 amatirimikitsa kuti titsendere chifupi ku machiritso ndi Yesaya 58:8 amatsimikidza kuti “kuchira kwathu kudzaonekera msanga msanga.”

Pa Yesaya 61:1 timaphunzira kuti Yesu anatumidzidwa kuzamanga osweka mtima. Izi zikukamba za machiritso a mkati, a maganizo.

Pa Yeremaya 8:14-15, 20-22 mkwiyo wa cthimo umakhudzana ndi matenda akuthup ndipo Yeremiya 15:18 akufotokoza momwe bala losapola limachidzidwira. Yermiya 14:14; 30:12-17; ndi 33:6 akutsimikidza kuti Mulungu ndi gwero la machiritso.

Ezekieli 30:12-13 ikufotokodza zilonda zosachitsdzika zomwe mankhwala sangachidze. Ndi machiritso a uzimu okhaomwe angachiritse mitundu ya zilonda izi. Ezekieli 34:4;16,21 ndi Zakaliya 11:6 muli machenjezo kwa azibusa (adzitsogoleri auzimu) omwe anyalanyaza nkhusa zodwala (anthu).

Danieli chaputala 4 ikukamba za kudwala kwa Mfumu Nedukadinezara ndi kuchira kwake. Hoseya 5:1 akuchenjeza zakuopsya kopita kwina kusaka machiritso ndipo Hoseya 6:1 ndi 7:1 akutsimikiza kuti Mulungu atha kuchiritse matenda akuthupi nd ku uzimu. Hoseya 11:3 pali mawu a Mulungu odandaulira Israyeli: “koma sanadziwa kuti ndinawachiritse.” Zolembedwa za Machiritso zamu Chipangano Chakale zikutsekedwa ndi lonjezano pa Malaki 4:2 kuti Yesu adzabwera ndi “machiritso mumapika Ake.”

MBIRI YA CHIPANGANO CHATSOPANO

Machiritso ndi mamasulidwe afotokozeredwa makuya mu Chipangano Chatsopano kudzera mu chitsanzo cha Yesu ndi Mpingo woyamba.

CHITSANZO CHA YESU:

Mu Chipangano Chatsopano, Yesu ndi chitsanzo cha machiritso ndi mchitidwe kwa okhulupirira. Utumiki wake wa machiritso ndi mamasulidwe ndi chitsanzo chomwe mukuyenera kutsatira mu utumiki wanu. Mwa mavesi 3,774 mu ma buku a Uthenga Wabwino, 484 akukamba za machiritso ndi kuuka kwa akufa. Mu Marko, mavesi 209 mwa mavesi 666 akukamba za zozizwa za Yesu.

Yesu anakamba za mau a Mulungu mu utumiki wake:

... Nsindicita kanthu kwa Ine ndekha, koma monga anandiphunzitsa Atate, ndilankhula izi. (Yohane 8:28)

Yesu anagwira ntchito ndi chifuniro cha Mulungu:

Pakuti ndinatsika Kumwamba, si kuti ndicite cifuniro canga, koma cifuniro ca iye amene anandituma Ine. (Yohane 6:38)

Tiyenera kugwira nchito za iye wondituma Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira nchito. (Yohane 9:4)

... Cakudya canga ndico kuti ndicite cifuniro ca iye amene anandituma Ine, ndi kutsiriza nchito yace. (Yohane 4:34)

Cholinga cha Yesu chinali chokaononga ntchito za Satana kuphatikiza tchimo, matenda ndi ukapolo:

... Kukacita ici Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge nchito za mdierekezi. (1 Yohane 3:8)

Ntchito yomwe Yesu anagwira inamutsangalatsa Atate:

... cifukwa ndicita Ine rimene zimkondweretsa iye nthawi zonse. (Yohane 8:29)

Izi zikutanthauza kuti mukamatumikira machiritso ndi mamasulidwe ngati Yesu, inu mukusangalatsa Atate, kulankhula Mau ake, Kuchita chifunira chake, ndi kuononga ntchito za woyipayo.

Pali maumboni ochuluka amu Chipangano Chatsopano pomwe Yesu anachiritsa aliyese yemwe analipo:

-Machitidwe 10:38

-Luka 4:40; 6:17-19; 9:11

-Mateyu 4:23-25; 9:6,35; 10:1; 12:15; 14:14,34-36

Yesu anachiritsa mitundu yambiriyamatenda:

-Khate

-Wambulu

-Osamva ndi kuyankhula

-Aziwanada

-Manja owuma (kupuwala kapena khate)

-Osaona

-Azofooka

-Kubwezeretsa khutu lomwe linadulidwa

-Kuukisa akufa

-Opundulidwa (monga mene yagwiritsidwira ntchito pa Marko 9:43)

Kukhuzidwa kunali chinthu comwe chimamulimbitsa mctima Yese mu utumiki wake wa machiritso (machitsanzo onani mavesi awa Mateyu 9:36; 12:9-13; 14:14; 18:27; 20:29-34; 29:34; Marko 1:41; 3:1-5; 5:19; Luka 6:6-10; 7:12-15; 10:33; 14:1-6 ndi Yohane 11:38-44).

Yesu anagwirita njira zosiyanasiyana pa machiritso. Nthawi zina amayitana odwala kwa iye (Marko 3:1-6). Nthawi zina odwala amamuyitana Yesu (onani nkhani ya kapolo wa Kenturiyo pa Mateyu 8:5-13; Luka 7:1-10 ndi machiritso a mwana wa Jairusi Mateyu 9:18-19; 23-26).

Yesu amathana ndi munthu yense, osati thupi mavuto athupi lokha. Anaphunzitsa kukhulukiridwa kwa machimo ndi machiritso limodzi. Nthawi zina amayamba wachiritsa, kenako kukhulukira macchimo (onani Luka 17:9 ndi Yohane 5:14). Nthawi zina amayamba kukhulukira machimo, kenako kuchiritsa (onani marko 2:1-12)

Nthawi zin machiritsa amachitika opanda chikhulupirira chamunthu odwala (koma sizinakambidwde):

- Lazalo: Yohane 11:1-44
- Khutu la kapolo wa mkulu wa nsembe: 22:50-15
- Wogwidwa ndi mzimu wonyansa ku Gerasi: Marko 5:1-20
- Munthu osalankhula ndi kumva: Marko 7:32-35
- Apongozi a Petulo: Luka 4:38-39
- Mwana wa mkazi wamasiye: Luka 7:12-15
- Munthu wa nkodo wouma: Marko 3:1-5
- Munthu obadwa osaona: Yohane 9:1-7
- Mwana wa Abrahamu: Luka 13:10-13
- Kaplolo wa Kentilyo: Mateyi 8:5-13
- Mwana wa mzaki waku Suro-Fonika: Mateyu 15:21-28
- Mwana wa Yairo: Marko 5:35-43

Nthawi zina machiritso amachitika chifukwa cha chikhulupiriro cha odwala:

- Amuna awiri osawona: Mateyu 9:27-31
- Wakhate: Mateyu 8:2-4; 20:29-34; Marko 1:40-44
- Akhate Khumi: Luka 17:11-19
- Amuna awiri osaona: Mateyu 20:29-34
- Batomeyo wosaona: Marko 10:446-42; Luka 18:35-43
- Mkazi wokhudza chofunda cha Yesu: Mateyu 9:20-22; Marko 5:25-34; Luka 8:43-48

Nthawi zina machiritso amachitika chifukwa cha chikhulupiriro cha anthu ena:

- Kapolo wa kentulyo: Mateyu 8:5-13
- Mwana wa mkulu wa mfumu: Yohane 4:46-53
- Amuna anayi omwe anabweresa muthu wopuwala: Mateyu 9:1-8; Marko 2:1-12; Luka 5:17-26
- Mwana wa mzaki waku Suro-Fonika: Mateyu 15:21-28
- Osamva chifukwa chakudzazidwa ndi mzimu woyipa: Mateyu 9:32-33

- Osamva/osalankhula, odzadzidwa ndi ziwanda: Maeteyu 12:22-23
- Mwana wa Yairo: Marko 5:35-43
- Mwamuna wosamva ndi kulankhula: Marko 7:32
- Mwamuna osaona: 8:22-26

Yesu amagwiritsa mawu osiyanasiyana pa kuchiritsa. Iye amalankhula mawu akulengeza okha

- Mwana wa Abrahamu: Luka 13:10-13

- Mwana wa mkulu wa mfumu: Yohane 4:46-53
- Batomeyo wosaona: Marko 10:44-42
- Amuna awiri osawona: Mateyu 9:27:31
- Kaplolo wa Kentilyo: Mateyi 8:5-13

Nthawi zina amalankhula Mawu aulamuliro:

- Mwamuna wamanjenje: Luka 5:17-26
- Mwana wa Yairo: Marko 5:22-24; 35-43

Nthawi zina Yesu amaphatikiza kulamula ndi kukhuza:

- Wakhate: Mateyu 8:2-4
- Amuna awiri osawona: Mateyu 9:27:31
- Apongozi a Petulo: Luka 4:38-39
- Mwamuna wosamva ndi kulankhula: Marko 7:32-35
- Mwana wa mkazi wamasiye: Luka 7:12-15
- Mwana wa Abrahamu: Luka 13:10-13

Nthawi zina Yesu amapemphera:

- Apongozi a Petulo: Luka 4:38-39
- Mwamuna wosamva ndi kulankhula: Marko 7:32-35
- Mwana wa mkazi wamasiye: Luka 7:12-15
- Lazalo: Yohane 11:1-44
- Munthu wa nkodo wouma: Marko 3:1-5

Nthawi zina sizinali zofunika kuti Yesua akepeze kwa munthu yemweakudwala. Amachiritisa ali kutali:

- Kaplolo wa Kentilyo: Mateyi 8:5-13
- Mwana wa mkulu wa mfumu: Yohane 4:46-53
- Mwana wa mzaki waku Suro-Fonika: Mateyu 15:21-28

Nthawi zambiri Yesu amawalamulika odwala kuti achite kanthu ngati mbali yamachiritso:

- Mwamuna wa dzanja lowuma anauzidwa kuti “atambasule dzanja lake”: Luka 6:6-11
- Mwamuna wopuwala pa thamanda la Betesda anauzidwa kuti “Tauka, yalula mphasa yako, nuyende”: Yohane 5:1-9
- Mkulu wa amfumu yemwe anali ndi mwana wodwala anauzidwa kuti “pita pa njira yako”: Yohane 4:46-54
- Akhate khume anawudzidwa kuti akazionetse okha kwa wa nsembe: Luka 17:11-19
- Mwamuna wosaona anawudzidwa kuti akasambe mu thamanda ya Siloma: Yohane 9:7

Yesu anatumikira machiritso pagulu (sinagogi) ndi malo obisika (kunyumba kwa anthu ndi kukumana ndi munthu mmodzi mmodzi)

Yesu anagwiritsa ntchito zachirendo ngati:

- Mate
- Dothi
- Dzala mmakutu
- Chofunda
- Kunsamba mmadzi

Nthawi zina odwala amamukhuza

- Mwana wa Yairo: Marko 5:35-43
- Khwimbi la anthu: Luka 6:17-19
- Khwimbi la anthu: Marko 3:10
- Laiyense yemwe anamukhuza: Marko 6:56

Nthawi zina amakhuza odwala

- Amuna awiri osaona: Mateyu 9:27-31
- Anthu amatenda osiyanasiyana: Luka 4:40
- Wakhate: Luka 5:13
- Mkazi wa mzimu wopeteka: Luka 13:10-13

Malangizo omwe Yesu anapereka potsatira machiritso anali otsiyanasiyana. Mwachitsanzo, apongozi a Peturo anadzuka pa kama nayamba kutumikira omwe anali mu nyumbamo. Yesu anayitanisa chakudya kuti chipatsidwe kwa mwana wa Yairo.

Machiritso a Yesu amachitikira ku malo osiyanasiyana:

- mkati kapena panja pa nyumba
- M'mitsonkhnao: m'misewu, m'mathamando, kumapiri, chombo
- Kumaliro
- Kumanda
- M'kachisi
- M'nkumano wachakudya
- Munjira yopita kumalo ena
- M'minda

Kumakhala mayankho osiyanasiyana ku zozizwitsa ndi machiritso

- Kudabwa
- Mantha a Mulungu
- Kustutsana
- Kukanidza ndi banja ndi akuluakulu a chipembedzo
- Ziwanda kukuwa
- Nkwiyo
- Kutchuka
- Kulemekeza Mulungu
- Kufunsa mafunso "Ichi ndi chani?"
- Kukambirana (lipoti ndi mphekesera)

-Chipulumutso cha banja lonse

Mwachidule, pomwe tikuona utumiki wa machiritso wa Yesu ngati chitsanzo cha utumiki wathu timapeza kuti Yesu analankhula Mawu a Mulungu ndi kuchita ntchito ya Mulungu mu utumiki wake. Machiritso ndi mamasulidwe anali mbali imodzi ya utumiki wake,

Nthawi zina Yesu amachiritsa aliyense alipo. Nthawi zina, amachiritsa anthu ena. anachiritsa matenda osiyanasiyana ndikugwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana. Nthawi zina machiritso amachitika opanda chikhulupiriro cha odwala. Nthawi zina amachitika chifukwa chachikhulupiriro cha odwala kapena abwenzi kapena achibale. Yesu amatumikira machiritso kwinakuli konse amapita ndipo utumiki wake unali wachifundo. Utumiki wake unalandiridwa mosiyanasiyana kuchokera kwa anthu ndi adzitsogoleri a chipembedzo ndi a ndale a nthawi imeneyo.

Yesu yemweyo akuyenda pakati pathu kupulumutsa ndi kuchiritsa matsiku ano. Kumbukirani kuti “Koma onse amene anamlandira iye... anali obadwa mwa Mulungu” (Yohane 1:12-13) ndipo “onse amene anamkhudza anaciritsidwa” (Marko 6:56).

CHITSANZO CHA MPINGO WOYAMBA:

Mpingo woyamba umaperekanso chitsanzo cha utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe. Ophunzira anaperekedwa ndi kutumizidwa ndi Yesu ku utumiki wa machiritso. Okhulupirira anachita monga momwe anawuziridwakuti achite, ndi kuyembekedzera Yesu kuchita zomwe analonjeza (machitsanzo onani Machitidwe 3:4-7; 8:4-8; 28:3-6).

Okhulupirira anamvetsetsa kuti mphamvu ndi ulamuliro wochiritsa siunali wawo koma wa Khristu (Machitidwe 3:4-7; 9:17-18). Pemphero inali mbali ya utumiki wawo wamachiritso (Machitidwe 4:23-21; 9:40-41; 28:8 ndi Yakobo 5:16). Iwo anali opembedzera komanso opempherera machiritso (Machitidwe 3:4-7 ndi Yakobo 5:14-16)

Zokumana za ophunzira zinachedwetsa machiritso. Werengani zitsanzo za Epafrodito pa Afilipi 2:25-30; Timoteyo pa 1 Timoteyo 5:23; ndi Trofimasi pa 2 Akorinto 8:18-22.

Ngati Yesu ophunzira anakumana mazunzo chifukwa cha utumiki wa machiritso (Machitidwe 4:3,29; 5:17-18; 6:9-15; 7:1-60).

Pali njira zambiri zosiyanasiyana za machiritso zomwe zalembedwa mu buku la Machitidwe:

- Kuyala manja: 5:12; 14:3; 19:11; 28:8
- Mawu kutsagazana ndi kuyala manja: Mwamuna wopuwala, 3:1-10
- Mawu kutsagazana ndi kutukula dzanja: Mwamuna wopuwala, 3:1-42; Maso a Paulo, 9:36-43
- Kulankhula Mawu (Kulamula mwa ulamuliro): Namwali wa mzimu wambwembwe, 16:18; Lustra opuwala, 14:10
- Pemphero: Maso a Paulo, 9:36—43; Bambo ake a Popliyo, 28:8-9
- Zofunda za pemphero: 19:11-12
- Chithunzithunzi: 5:12-16
- Kufungatira: 19:12

- Kuzungulira: 14:19-20
- Sanakambepo: 14:19-20
- Mawu ndi kulamulira kuti pakachitidwe kanthu: Ayenesi, 9:33-34, Mwamuna wopuwala, chaputala 3

Nthawi zina machiritso amachitika chifukwa:

- Odwala anatengapo gawo: Mwamuna opuwala pa khomo la kachisi, Machitidwe 3:3
- Abwenzi anatengapo gawo: Tabita, Machitidwe 9:38
- Atumwi anatengapo gawo:

-Peturo:	Eneya ku Lidiya:	Machitidwe 9:34
-Paulo:	Opuwala ku Listra:	Machitidwe 14:9
-Paulo:	Namwali wa mzimu wambwembwe:	Machitidwe 16:18
-Paulo:	Utikasi:	Machitidwe 20:10
-Paulo:	Atate ake a Popliyo:	Machitidwe 28:8

Okhulupirira kutumikira kwa munthu modzi modzi. Onani tchati iri munsiyi:

Machiritso A Modzi Modzi Ndi Ophunzira

Chochitika	Machitidwe	Mtundu
Machiritso a opuwala opepmphetsa	3:1-4:22	Kuthupi
Maso a Paulo	9:10-19; 22:10-21	Kuthupi
Peturo achiritsa Eneya	9:32-35	Kuthupi
Peturo achiritsa Dokasi (Tabita)	9:36-43	Kuukisa wakufa
Mwamuna wopuwala kuu Listra	14:8-18	kuthupi
Paulo ku Listra	14:19-20	Kuthupi
Namwali wa mzimu wambwembwe	16:16-40	Ziwanda
Utiko	20:7-12	Kuukisa wakufa
Paulo alumidwa ndi njika	28:3-6	Kuthupi
Atate ake a Popliyo	28:8-9	Kuthupi

Okhulupirira kutumkira ku gulu la anthu. Onanii tchati yotsatirayi:

Machiritso A Pamodzi A Ophunzira

	Machitidwe
Zozizwa ndi zizindikira zochuluka	2:42-47
Pemphero la kulimbika mtima ndi zizindikiro za machiritso	4:23-31
Ambiri anachiritsidwa ku Yerusalemu	5:12-26
Stefano anchitsa zozizwitsa zambiri	6:8-15
Filipo anachiritso ochuluka ku Samariya	8:5-25
Paulo ndi Banabasi anachita zizindikiro ndi zozizwitsa	14:3
Paulo achiritsa odwala ku Aefeso	19:11-12
Odwala achiritsidwa ku Mata	28:8-9

Panali mitundu yambiri ya matenda yomwe inachiritsidwa. Onani tchati yotsatirayi:

Mitundu Ya Matenda Yomwe Inachiritsidwa

		Machitidwe
Malungo ndi kamwaza	Atate ake a Popliyo	28:8
Khungu	Paul	9:8
Kuvulala mutu (kumwalira)	Utiko	20:9
Matenda aku imfa	Tabita	9:37
Manyenje	Eneya	9:33
Kupunduka	opunduka ambiri	3:2; 8:7; 14:8
Namwali wa mzimu wambwembwe	Filipi	16:16-40s
Kulumidwa ndi njoka	Paulo	28:3-6

(Matenda ya matanda yambiri yomwe sinakambidwe inachiritsidwanso mu chigulugulu)

Machiritso nthawi zina amachitika poyankha pempho:

- La mwamuna wopunduka Machitidwe 3:2
- La abwenzi (Tabita) Machitidwe 9:39

Machiritso amachitika pakuyankha chotsowa:

- Eneya wa manjenje Machitidwe 9:33
- Utiko Machitidwe 20:10
- Atate ake a Popliyo Machitidwe 28:8
- Odwala waku Mata Machitidwe 28:9

Machiritso amachitika chifukwa cha mayankhidwe a chikhulupiriro:

- Wopuwala waku Lustra Machitidwe 14:9

Machiritso amachitika pakuyankha zosautsa:

- Namwali wa mzimu wambwembwe Machitidwe 16:18

Kuchokera mu zitsanzo za ophunzira taphunzira analamulidwa ndi kutumizidwa ndi Yesu ku utumiki wamachiritso. Anamvetsetsa kuti mphamvu ndi ulamuliro zinali zochokera kwa Yesu. Pemphero linali mbali ya utumiki wawo wamachiritso ndipo anakumana ndi machiritso apang'onopan'ono ndi apompompo.

Monga Yesu, anakumana ndi mazunzo chifukwa cha utumiki wawo wamachiritso. Amagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana za machiritso ndi kuthana ndi matenda osiyanasiyana. Nthawi zina machiritso amachitika chifukwa odwala amatengapo kanthu, kapena atumwi kutengapo kanthu. Ophunzira amatumikira ku munthu modzi modzi ndi ku gulu.

Kuchokera ku zolemba za mu Chipangano Chatsopanao, zikutsonyezeratu kuti zozizwa, machiritso, ndi mamasulidwe sizinathe ndi utumiki wa Yesu. Zizindikiro izi zinawatsata “iwo okhulupirira.”

MACHIRITSO NDI NSEMBE

Tikufuna tione chitsanzo china chofunika kwambiri cha mu Baibulo mwatsatanetsatane:

Zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kuzenza zisoni zathu; koma ife tinamuvesa wokhomedwa wokanthidwa ndi Mulungu, ndi wobvutidwa.

Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natunduzidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. (Yesaya 53:4-5)

Yesaya 53 ndi chaputala cha uneneri chokamba za Yesu Khristu. Mavesi a 4 ndi 5 akulumikiza machiritso ndi nsembe ya Yesu ya imfa yake pa mtanda. Pakugwiritsa mawu oti “zoondi” mu chaputala ichi, omwe ali mawu otsimikiza, akukamba za chipulumutso chathu ndi machiritso.

Tchimo ndi matenda ndi zoyipa za Satana. Chipulumutso ndi machiritso ndi chipulumutso choperekedwa ndi Mulungu. Pasanafike Pakavale anthu amapulumsidwa ndi kuchiritsidwa pokuyang’ana ndi chikhulupiriro. Kenako, chipulumutso ndi machiritso amabwera pakuyang’ananso ndi chikhulupiriro.

Matenda ndi imfa zinalowa ndi tchimo ndipo ndi mphoto ya zoipa, ndipo chipulumutso chikuyenera kupezeka mu nsembe. Yesu ananyamula nthenda zanu ndi kutenda madwale pa nthawi imodzi ndi nthawi imodzinso ananyamula machimo anu.

kotero kuti cikwaniridwe conenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti, Iye yekha anatenga zofoka zathu, Nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:17)

Mulungu anyiika machimo ndi matenda pa Yesu ngati nsembe. Peturo akulankhula za chipulumutso ndi machiritso kukhala chilungamo chokwaniritsidwa:

Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, titafa kumacimo, tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; ameneyo mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo. (1 Petro 2:24)

Pakuti Yesu ananyamula machimo anu, chikuyenera kukhala chifuniro cha Mulungu kukupulumutsani mukabwera kwa iye. Pakuti ananyamula nthenda zanu, zikuyeneratso kukhala chifuniro chake chokuchiritsani mukabwera kwa iye. Mulungu yemweyo yemwe amakhululuka machimo anu onse ndi Mulungu yemweyo amene machiritso nthenda zanu zonse.

Lemekeza Yehova, moyo wanga, Ndi kusaiwala zokoma zace zonse aticitirazi: Amene akhululukira mphulupulu zako zonse; Naciritsa nthenda zako zonse. (Masalmo 103:2-3)

Dzina la chipulumutso “Yehova-tsidkenu” limabvumbulutsa chipulumutso cha Mulungu cha moyo wanu. Dzina la chipulumutso la “Yehova-rapha” imabvumbulutsa machiritso a Mulungu.

Mawu oti “kupulumutsa” pa Aroma 10:9 ndi mawu omwewo omwe anagwiritsidwa nctito ndi Marko pamene anati “onse amene anamkhudza anaciritsidwa.” Mawu ach Greek “sozo”

ogwiritsidwa mu ndimezi akutanthauza kupulumutsa kuchokera ku tchimo ndi mphoto yake. Matenda ndi mbali yam photo, ndiye chipulumutso ndi mbali ya nsembe ya tchimo.

Pamene nsembe ya Yesu ikutsimikizira ungwiro wa okhulupirira, ungwiro wa kuthupi ndi uzimu omapitirira. Okhulupirira amapitirira kukumana ndi maupo a tchimo ndi matenda. Phindu lake lenileni la nsembe ya Yesu ndiyote ibvumbulutsidwe:

Amene musungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa cikhulupiriro, kufikira cipulumutso cokonzeka kukabvumbulutsidwa nthawi yotsiriza. (1 Petro 1:5)

Phindu la chipulumutso lomwe likuyenera kubvumbulutsidwa ndi ungwiro wa kuthupi ndi uzimu wa muyaya.

Pamene Yesu anafa pa mtanda kodi anatenga machimo ako onse? Kodi ngati okhulupirira, mumalimbanabe ndi tchimo? Chomwecho ndi choona ndi matenda. Yesu anafa chifukwa cha matenda anu, koma ngati mukukhalabe m'dziko lopanda ungwiro ndipo Satana sanamangidwebe, mukuyenera mumenyana naye nkhondo.

Pali chipulumutsa chakale, chatsopano, ndi chamstogolo:

- Chakale: Munapulumsidwa ku mphoto la uchimo omwe munachita m'mbuyomo
- Chatsopano: Mwapulumutsidwa ku mphamvu ya tchimo yapano.
- Chamstogolo: Mudzapulumutsidwa ku machimo a mtsogolo (muyaya).

Chomwechinso ndi zooni ndi machiritso. Inu munapulumsidwa ku mphoto ya matenda chifukwa cha tchimo. Mutha kugonjetsa mphamvu ya matenda mu nthawi ino ndi kupulumutsidwa kukuozeke kwa matenda mpaka muyaya.

Poti machiritso ndi phindu la nsembe, mukuyenera kumulandira Yesu osati ngati Mpulumutsi chabe, komanso ngati Mchiritsa. Kodi akutetezani bwanji ku tchimo ngati inu simunamulandire ngati Mpulumutsi? Kodi akutetezani bwanji ku matenda ngati inu simunamulandire ngati Mchiritsi?

KUTUMIZIDWA KU GEHENA

Yesu analamulira ophunzira ake kulalikira ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu ndi kuonetsera mphamvu yake. Onani tchati yotsatirayi ndipo muonentso chitsanzo chake mu Baibulo

	Mateyu	Marko	Luka	Machitidwe
Kutumiza 12	10:1-42		6:7-13 9:1-6	
Kutumiza 70			10:1-24	
Mphamvu yomanga ndi kumasula	16:17-19			
Kutumizidwa komaliza	28:16-20	16:14-20	24:44-53	1:1-11

Kuchokera kuzolembedwa za Mateyu 10:1-42; Marko 6:7-13; ndi Luka 9:1-6, apa pali ndandanda wa malangizo operekedwa kwa ophunzira 12 otumizidwa:

-Pitani awiri awiri

- Pitani ku Israyeli
- Kalalikireni uthenga wa Ufumu, kuphatikizirapo kulapa
- Kachiritseni matenda ndi kuchiritsa mitundu yonse ya madwale
- Kaukiseni akufa
- Kayereseni a khate
- Katuluseni ziwanda
- Musachedwe ndikusamala zovala kapena chuma kuti mupite'
- Mwaulere mwalandira, mwaulere perekani
- Mphamvu ndi ulamuliro zinaperekedwa zogonjetsa mizimu yoyipa ndi Satana

Luka 9:6 ndi Marko 6:112-13 akukamba zotsatira za utumiki wawo.

Pa Luka 10:1-24, timawerenga kutumizidwa kwa Ophunzira 70. Malangizo omwe anaperekedwa anali:

- Pitani pa njira yanu: Utumiki siunali wa Israyeli okha. Amayenera kupita ku mzinda wina uli wonse angapite.
- Kalalikireni uthenga wa Ufumu.
- Kachiritseni odwala.
- Anapatsidwa mphamvu yoponda njoka, pa phamvu ina iriyonse ya mdaniyo, ndipo palibe chomwe chingawapweteke.

Zotsatira za utumiki wawo zarembedwa pa Luka 10:17 ndi kuyankha kwa Yesu pa Luka 10:18-20.

Kutumiza komaliza kwa Yesu ku ophunzira ake kwalembedwa pa Mateyu 28:18-20; Marko 16:16-20 (zotchedwa kuti Utumiki Waukulu); ndi Luka 24:22-53. Kutumizidwa uku ndikoti kukuyenera kukwaniritsidwa ndi okhulupirira onse. Kuchokera ku zitsanzo zonse pamodzi, nawa malangizo onse:

- Pitani inu ndi kukaphunzitsa mitundu yonse, ku dziko lonse, kwa mitundu yonse, kuyabira ku Yerusalemu; kukafikira ku cholengedwa chinachiri chonse.
- Kulalikira kulapa ndi kukhululukidwa cha machimo mu dzina lake.
- Kuphunzisa Uthenga Wabwino, pakutha pa kutembenuka kuphunzisa otembenuka kuti atsunge zinthu zonse zimene Yesu analamulira.
- Mphamvu ya ntchitoyi yalonjezedwa. Zizindikiro izi zizawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano; adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteke; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzachira.
- Yesu adzakhala ndi onse omwe angsamagwire ntchito ya utumiki.

Aliyense obadwa mwatsopano nchoonadi, akuyenera kutengapo gawo pa ntchito ya utumiki yofikira mitundu yonse ndi Uthenga Wabwino wa chipulumutso, machiritso ndi mamasulidwe. Utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe si wochitakusanknidwa ndi Mpingo. Ndi mbali imodzi yofuninikira ya Utumiki Waukulu.

MAFUNGULO A MU UFUMU

Mu Chipangano Chatsopano Yesu anapereka zoonadi zambiri za “mufungulo” kuti timvetsetse Ufumu wa Mulungu. Atatu a mafungulo ali ofunikira kwambiri pa kutumikira ndi kulandira machiritso. Fungulo **loyamba** ndilakuti ngati cholinga chanu chachikuli chiri chiri Ufumu wa Mulungu, zinthu zonse zofunikira (kuphatikizira machiritso) zizaperekedwa:

Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)

Fungulo **lachiwiri** ndirakuti kuti mulandire, mukuyenera kupereka:

Patsani, ndipo kudzapatsidwa kwa inu... (Luka 6:38)

Ngati mukufuna mulandire machiritso, yambani utumikira machiritso. Pamene mukupereka, murandira. Abrahamu anpemphepera mkazi wosabereka wa Abimeleki ndipo anachiritsidwa ingakhale mzaki wake Sara, anali osabereka. Kenako, Sara anabara Isaki.

Fungulo **lachitatu** lofunikira kwambiri ndirakuti palibe chomulaka Mulungu:

Koma iye anati, Zinthu zosatheka ndi anthu zitheka ndi Mulungu. (Luka 18:27)

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lemabani lonjezo la machiritso.

2. Lembani mwachidule ziphunzitso za Muchipangano Chakale za machiritso.

3. Kugwiritsa ntchito zitsanzo za Yesu ndi Mpingo woyamba, lembani mwachidule ziphunzitso za machiritso amu Chipangano Chatsopano.

4. Kuchokera m'malembo, tsimikizani kuti machiritso ndi phindu la nsembe ya Yesu.

5. Lembani mwachidule Utumiki Waukulu poyerekezera ndi machiritso ndi mamsulidwe.

6. Lembani zitsanzo za m'Baibulo zomwe zimatsimikidza kuti okhulupirira onse azitengapo ngawo pa machiritso ndi mamsulidwe.

7. Kodi mafungulo atatu a Ufumu yomwe imakhuzana ndi machiritso.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Gwiritsani ntchito zolembedwa ku mapeo a nukuli kuti mupitireize phunziro lanu la mfundo za machiritso za m’Baibulo. Mukamaliza kuwerenga, mupitirize kukulitsa phunzirori pakuonjezera zolemba zanu.
2. Kaganiziridwe kathu ka machiritso a mu Baibulo sikakhala kopindula ngati sitiganizira za zolephera za omwe anatengapo gawo mu utumika wa machiritso. Nthawi zonse kumbukirani, mukumathana ndi zinthu zimenezo, kathandauziridwe ka malembo a m’Baibulo kali pa malonjezano ndi ziphunzitso zake, osati zinthu zomwe anthu akumana zano. Nthawi zina munthu amatha kulephera—koma osati Mulungu.

Epafrodito (Afilipo 2:25-27) anatsala pang’ono kufa chifukwa cha matenda. Iye sanakumane ndi machiritso a pompopompo, ingakhale zitha kuganiziridwa kuti Paulo anantumikira iye. Epafrodito pamapeto pake anachiritsidwa. Zindikirani kuti machiritso enieni amachokera kwa Mulungu, kaya apompopompo, pango’onopang’ono kapena machiritso achirengedwe. Inu simunalephere chifukwa machiritso a pompopompo sanaoneke.

2 Timoteyo 4:20 imakamba zomusiya munthu wodwala wotchedwa Trifomo. Nkhani yake ndiyayifupi. Paulo anamusiya ali odwala, koma sitinauzidwe ngati anachiritsidwa.

Mateyu 17:14-21; Marko 9:14-29; ndi Luka 9:37-45 imakamba zakulephera kwa ophunzira kutumikira mamasulidwe kwa mnyamata yemwe anali ndi ziwanda. Makambidwe ankhanayi kuchokera mu mabuku onse atatu zikuonetsera kuti anali:

- Odwala khunyu
- Ozunzika kwambiri
- Okugwa kawirikawiri pa moto ndi m’madzi
- Ong’amba iye ndi ochita thubvu
- Osamva
- Okukuta mano
- Onyololoka kuyambira umwana

Malingana ndi Yesu, ophunzira analephera chifukwa cha kusakhulupirira kwawo ndikuti mtumbu wa chiwanda ichi umatuluka pokhapokha pakupemphera ndi pkutsala kudya. Komanso pakhoza kukukhala kuti panali kusakhulupirira, chifukwa ophunzira anazungulidwa ndi kufunsana mafunso ndi azitsogoleri a chipembezo cha nthawi imeneyo. Nkhaniyi imaonetseranso kuti pali mitundu yosiyanasiyana ya mphamvu za ziwana, zina zamphamvu kwambiri kuponsa zinzake. Ikuonetseranso kuti kuthana ndi mitundu yaziwanda izi pamafunikira kukonzekera bwino mu uzimu.

Umu ndi momwe Yesu anathanira ndi zinthuzo. Poyamba anafunsa atate a mnyamatayo, “kodi Chimenechi chinayamba kumugwira liti? Ndipo anati chinayamba ali mwana. Yesu anadzudzula mzimu woyipa ndikuchiuza kuti chituluke ndi kusalowanso mwa iye. Mzimu woyipawo unang’amba nagwa pansu ndipo anakhala ngati wakufa. Yesu anatchula mzimuwo wosalankhula

ndi wogontha. Ena anaona ngati mwanayo wafa, koma Yesu anamgwira dzanja lake nanyamula. Mzimu unachoka, ndipo anachiritsidwa.

Chenjezo pa zinthu izi: mukufenera kukhala otsamalitsa osatenga kuti kusalankhula ndi kugontha ndi/kapena iwo onse okugwa khunyu ali ndi ziwanda. Onse osalankhula ndi ogontha si aziwanda. Atha kukhala kuti anadwalapo kwambambiri kapena anachita ngozi.

Komanso pali matenda ena otcedwa “khuny” omwe sali kuzazidwa ndi ziwanda. Zizindikiro za khuny ndizofanana (onani chart chiri mutsimu). Khunyu ndi chizindikira kuti ubongo wa munthu sukugwira ntchito yake bwino bwino. Itha kukhala ndi zoyambisa zosiyanasiyana. Alipo anthu ena omwe amadwala nkunyu omwe gwero lake litha kuzindikiridwa (chitha kukhala chotopa chamu ubongo) ndi kuchizika ndi kuchipatala. Mwa ena gwero lake siriziwika:

Khunyu

Nthawi zambiri imayamba kuumwana
Imayamba mwadzidzidzi
Kukhala ngati wakufa
Kuvulala kawiri kawiri
Kuwodzera ndi kukhala otopa

Khunyu la mwana

Inayamba kuumwana
Imayamba mwadzidzidzi
Mwanayo anakhala ngati wakufa
Amaziponya pa moto ndi m’madzi
Nyamatayo anali otopa...
Ndipo ena anawona ngati wafa

3. Machiritso ndi opezeka osati ku matenda okhuza thupi okha. Mu m’Baibulo timapeza:

- Kuchiritso a mtimwa wosweka: Salimo 147:3
- Kuchiritso moyo wa uchimo: Salimo 41:4
- Kuchiritso obwerera m’mbuyo: Yeremiya 3:22; Hoseya 14:4
- Madzi amachiritso: 2 Mafumu 2:21,22; Ezekiel 47:8,9
- Kuchiritso anthu aku Israyeli ndi mzinda wa Yerusalemu: 2 Mbiri 7:14; 30:20; Yesaya 30:26; 57:18; Hoseya 11:3
- Lonjezo lochiritso Igipito ndi anthu amitundu: Yesaya 19:22; 57:19

4. Chikhalidwe cha patatu cha munthu cha thupi, moyo, ndi mzimu chakambidwapo mu phunzirori. Kuti muphunzire zambiri za phunzori, werengani mawu a “thupi, moyo, ndi mzimu” mu Baubulo. Ndizofunikira kuti inu memvetsetse thupi, moyo, ndi mzimu wanu ndi ntchito zawo pomwe mukufuna kutumikira ndi kulandira machiritso.

5. Nawa ndandanda wa Malembo a machiritso ndi mamasulidwe:

UMBONI OCHOKERA MU CHIPANGANO CHAKALE

Genesis 17:18-19: Mulungu analonjeza kuchiritso kusabereka kwa Sara.

Genesis 20:17: Mulungu anachiritso Abimereki

Eksodo 4:6-7: Dzanja la Mose la khate

Eksodo 15:25-26 Mulungu awulula dzina lake ngati “Yehova-Rapha” kutathauza kuti “Ambuye wakuchiritsa.” Ana lonjeza kuti palibe nthenda iriyonse imene anaika pa Aaigupto imene izabwere pa Aaisreeli.

Levitiko 13:1-46: Mulungu analonjeza kuchotsa matenda pa anthu ake.

Levitiko 14:1-32: Malamulo okhudzana ndi khate

Levitiko 15:1-33: Malamulo amachiritso

Levitiko 16:29-30: Kuchiritsidwa kwamachimo

Numeri 12:1-15: Khate la Miriam ndi Aaron

Numeri 16:41-50: Muliri ukhudza Aisraeli

Numeri 21:5-9: Kuchiritsidwa kuchokera kuchifanifani cha njoka yamkuwa

Dueteronomo 7:15: Kumvera kwa Mulungu kumabweretsa moyo wathanzi

Dueteronomo 28: Matenda obwera chifukwa chosamvera Mulungu

Dueteronomo 29:22 Mulungu anaika matenda padziko

Dueteronomo 30:20: Mulungu ndi moyo ndi ochulukitsa masiku

Dueteronomo 32:39: Mulungu amakatha ndi kuchiritsa

Dueteronomo 7:15; 28:60: Matenda pa Aaigupto

Yoswa 5:8: Kuchiritsidwa kwachilengedwe kubala lamdulidwe

1 Samueli 6:3: Chopereka chopalamula chimabweretsa machiritso

1 Samueli 16:14-23: Mzimu woyipa umuzuza Sauli

1 Mafumu 5:23; 2 Mbiri 16:12: Matenda amapazi

1 Mafumu 8:37-40: Miliri mdziko

1 Mafumu 13:4-6: Munthu wadza lopuwala

1 Mafumu 17:17-24: Eliya aukitsa mwana kwa akufa. (Mtumwi ndi uthenga amatsimikizidwa chifukwa cha machiritso)

2 Mafumu 1:2; 8:8-9: Kodi ndizachira ku mnthenda imeneyi?

2 Mafumu 2:19-22: Kuchiritsidwa kwa madzi ndi Elisha

2 Mafumu 4:8-37: Kuukitsidwa kwa mwana waku Sunemu

2 Mafumu 5:1-14: Kuchiritsidwa kwa Namani

2 Mafumu 13:14,21: Elisa adwala nthenda yomutengera kuimfa

2 Mafumu 20:1-11: Kudwala kwa Hezekiya

2 Mbiri 6:26-31: Pemphero lakulapa ndi madwale

2 Mbiri 7:14: “Ndizachiritsa nthaka yawo”

2 Mbiri 16:12: Munthu wathenda yaikulu safuna Mulungu

2 Mbiri 20:9: Mulungu amava tikafuula muzowawa zathu

2 Mbiri 21:12-30: Nthenda yosachiritsika ya matumbo

2 Mbiri 24:25: Nthenda yotchulidwa kuti yauikulu

2 Mbiri 26:19: Khate la Uziya

2 Mbiri 30:20: Kuchiritsidwa kwa anthu ndi pemphero la Hezekiya

2 Mbiri 32:24-26: Kudwala kwa Hezekiya

Yobu 1-2: ma chaputala awa amawonetsa chiyambi cha mamvuto a Yobu, kuphatikizapo kudwala kwake

Yobu 5:18; 30:18: Yobu ayakhulapo za matenda ake

Masalimo 6:2-3: “Mulungu ndi chizeni”

Masalimo 27:1: “Mulungu ndiye mphamvu ya moyo wanga”

Masalimo 30:2: “Ndinafuula ndipo Inu munandichiza”

Masalimo 32:3-5 Kuvomereza tchimo kumabweretsa machiritso

Masalimo 34:19-20: “Zowawa za olungama ndi zochuluka, koma Mulungu amamulanditsa iye kwa iwo”

Masalimo 38:3,7: Mkwiyi ndi tchimo zimawononga moyo wanu; nthenda imatchulidwa kuti “chowoletsa”

Masalimo 41:1-8: “Chizani moyo wanga popeza ndakuchimwirani. “Nthenda ikutchulidwa kuti choipa”

Masalimo 42:11; 43:5: Mulungu ndi thanzi wanthu

Masalimo 55:1-2: Kuchiritsidwa kwa mzimu wakugwa

Masalimo 60:2: “Kuchiza kwazolakwa zadziko”

Masalimo 67:2: “Kuti njira zanu zidziwike pa dziko la pansu, kupukulutsa kwanu kochiza pakati pa mafuko”

Masalimo 72:13: Ndife ofooka ndi chisoni

Masalimo 91:9, 10: “Palibe mulire omwe uzafike komwe umakhala”

Masalimo 103:1-5: “Osaiwalira zomwe wakuchitira... Ndiamene wachiritisa nthenda zako zonse”

Masalimo 105:37: Israeli anabwera wabwinobwino opanda modzi yemwe ovulala. Anthu okwana 3,000,000 onse anali bwino ndi amphamvu.

Masalimo 107:17-20: “Anatumiza Mau Ake ndipo anachiritso iwo”

Masalimo 119:25-28: Timalimbikitsidwa ndi Mau

Masalimo 119: 67: “Poyamba nazuzidwa, ndipo nasochera”

Masalimo 147:3: “Amene amachiza nthenda zako zonse.” Machiritso amtima osweka.

Masalimo 105:37: “Anatulutsa onse...Palibe ndi modzi yemwe amene anamwalira.

Miyambo 3:7-8: Mmene tingakhalire moyo wathanzi

Miyambo 4:20-23: Zinthu zokhudzana moyo zimasokonekera ndi zamuntima. Malonjezano a Mulungu ndi moyo kwa onse amane awapeza ndipo ndi nthanzi kuthupi lawo.

Miyambo 12:18: Lirime la munthu wa nzeru limabweretsa machiritso

Miyambo 13:17: Kazembe wokhulupirika amafanizidwa ndi moyo wathanzi

Miyambo 15:4, 30: Lilime lowongoka ndi moyo; uthenga wabwino umakoza moyo

Miyambo 16:24: Mau a Mulungu amabweretsa moyo kumafupa

Miyambo 17:22: Mzimu wosweka omasokoneza mafupa

Mlaliki 3:3: Pali nthawi yake yochiza

Mlaliki 17:22: Chisoni ndi mkwiyo zimabweretsa matenda

Yesaya 6:10: Kumvetsetsa kukambira, machiritso

Yesaya 19:22: Pamene Mulungu wapephedwa, Amachiritisa

Yesaya 33:3-4: Uneneri wamachiritso kukhala mbali imodzi ya Ufumu wa Mulungu

Yesaya 35:5-6: Machiritso m'tsogolo

Yesaya 38:1-12: Kudwala kwa Hezekiya ndikubwerera kwake kumoyo wathazi

Yesaya 53:5: Talonjezedwa machiritso ndi mamasuridwe kupyolera mu imfa ya Yesu

Yesaya 57:18-19: Senderani chifupi ndimachits

Yesaya 58:8: Machiritso azatumphuka

Yesaya 61:1: Yesu anatumidwa kuti azamange mitima yosweka

Yeremiya 3:22: Mulungu amachiritisa onse obwerera m'mbuyo

Yeremiya 8:14-15; 20-22: Nthawi yamachiritso. Ululu wa tchimo umakhudza nthanzi lo la thupi

Yeremiya 15:18: Mmene tingathanirane ndi matenda osachizika

Yeremiya 14:19: Kodi palibe machiritso anthu?

Yeremiya 17:14: “Ndichizeni ndipo ndizachiritsika”

Yeremiya 30:12-17: Mulungu azabwezeretsa nthazi

Yeremiya 33:6: “Ndizachiritsa iwo”

Yeremiya 46:11: “Palibe kuchira kwawo”

Yeremiya 51:8-9: Kuchiritsidwa kwa Babulo

Maliro 2:13: “Ndindani amene angachiritso inu”

Maliro 2:33: “Mulungu samalanga mofuna”

Ezekieli 14:19: “Kodi kulibe machiritso anthu?”

Ezekieli 17:14: “Ndichizeni ndipo ndizachizika”

Ezekieli 30:17: “Zabwezeretsaso nthanzi”

Ezekieli 30:12-13: Zilonda zosachiritsika makhwala sangachiritse

Ezekieli 30:21: Chomwe Mulungu waphwasula palibe yemwe angachiritse

Ezekieli 33:6: “Ndizawachiritso iwo”

Ezekieli 34:4, 16, 21: Chenjezo kwa abusa omwe sanachiritsidwe

Ezekieli 47:8-12: Kuchiritsidwa kwa madzi

Danieli 4:34,36: Kuchiritsidwa kwa Nebukatineza

Hoseya 5:13: Kupita kwina chifukwa chamachiritso. Munthu sangachiritse bala lobweretsedwa ndi Mulungu.

Hoseya 6:1: “Yense yemwe wang’ambika ndipo Iye azamuchiza”

Hoseya 7:1: Machiritso kwa Aaisraeli

Hoseya 11:3: “Samazindikira kuti Ndinawachiritsa”

Hoseya 14:4: “Zachiritsa kubwerera mbuyo kwawo”

Nahumu 3:19: Nyengo yowawitsa

Zakariya 11:16: Chenjezo kwa abusa omwe samachiritsa

Malaki 4:2: Machiritso mmapiko Mwake

UMBONI WAMU CHIPANGANO CHATSOPANO

Mateyu 8: 13: Malo okumanirana amaika nthawi

Mateyu 8:17: Yesu anasenza matenda athu

Mateyu 10:1: Mphamvu pa matenda ndi ziwanda zapatsidwa kwa okphunzira Ake

Mateyu 18:19-12: Pomwe awiri amvomerezana amalandira chomwe apempha

Marko 2:17: Khristu anabwera kuzachiritsa ochimwa

Marko 3:15-17: Khristu anapereka mphamvu yochiza odwala

Marko 4:18-19: Kuchiritsa inali mbali imodzi yakudzodzedwa kwadzedwa kwa Yesu ndipo anatomizidwa kuzachiritsa

Marko 11:24: Ngati tikhulupirira pamene tipemphera (osati mukalandira), muzalandira.

Marko 16:18: Mudzina la Yesu okhulupirira azachiritsa ndi kutulutsa ziwanda

Luka 5:31: Odwala amafuna sing'anga

Luka 7:6: Kusayenera kunawonekera ndi Yesu ngati chikhulupiriro

Luka 17:6: Chikhulupiriro chochepa chikhoza kubweretsa zotsatira zazikulu

Luka 18:7-8: Musamasiye yankho lanu lisanafike

(Nkhani ya Danielo mu Chipangano Chakale imawonetseraso kupambana kwapemphero: Mulungu anamumva Danielo patsiku loyamba lomwe, koma satana anagwirigwira kwa masiku 21)

Yohane 6:53-58: Thupi ndi mwazi wa Yesu umabweretsa moyo

Yohane 10:10: Yesu anabwera kuti tikhale ndi moyo. Satana anabwera kuzampha, kuba ndi kuwononga

Yohane 11:1-45: Nthenda yosachizika pano imapereka njira kuchozizwa chapamwamba

Yohane 15:7: Ntchito zimene Yesu anachita, tikuyenera kuzichitanso

Yohane 16:24: Pemphani mu dzina Lake ndipo muzalandira.

Aroma 2:4: Chifundo cha Mulungu chimatsogolera kukulapa. (Dziwani kuti matenda satsogolera kukulapa; ndi kukoma mtima kwa Mulungu basi)

2 Akorinto 4:16: Munthu wanthu wakunja amawonongeka, koma munthu wamkati akhoza kukozedwaso

Aefeso 3:20-21: Mulungu ali ndimphamvu yogwira ntchito mwa ife pazonse zimene timapempha kapene kuganiza

Afilipi 2:25-27: Kudwala kwa Epafrodito

Akolose 4:14: Luka, sing'anga, anali mbali imodzi ya Paulo kufalitsa Uthenga

2 Timoteo 4:20: Trofimo nkhani yake irimwachidule, zohepa zokha ndizimene zingapezeke kuchokera muzimenezi. Paulo sikuti anamusiya akudwala, koma sitinauzidwe ngati anachiritsidwa pompo kapena pang'onopang'ono, kapena kuti chinaretsa machiritso ake nchani.

Ahebri 4:15: Amakhudzika ndi zowawa zanthu

Ahebri 11:1: Chikhulupiriro ndiumboni wa zinthu (machiritso) zosawoneka

Yakobo 1:6: Tikuyenera kupempha ndi chikhulupiriro osati kugwedezeke

Yakobo 1:17: Mphatso ina iriyonse yabwino (machiritso) imachokera kwa Mulungu

Yakobo 5:14-15: Kuitana akulu ampingo kuzakudzodzi ndi mafuta, pemphero lachikhulupiriro, machiritso ndi kukhululuka

1 Petro 2:24: Tinachiritsidwa ndi mabala Ake

1 Yohane 3:22: Chilichonse tipempha tikhoza kulandira ngati tiriomvera

3 Yohane 1:2: Moyo wanthazi umagwirizan ndi nyengo ya moyo wanu

Marko 7:36; 8:26; Mateyu 8:4: Musamaseweretse machiritso

Chibvumbulutso 20:2-3: Pamene satana azamangidwa, sipazakhalanso matenda ndi imfa

Chibvumbulutso 21:4: Machiritso omaliza: Sikuzakhalanso machiritso ndi imfa

CHAPUTALA 9

ZOLINGA ZA MACHIRITSO

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kudzindikira zolinga 9 za machiritso

LONJEZO LA MACHIRITSO:

...ndipo Iye anaturutsa mizimuyo ndi mau, naciritsa akudwala onse; kotero kuti cikwaniridwe conenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti, Iye yekha anatenga zofoka zathu, Nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:16-17)

CHIYAMBI

Cholinga cha chidziwikire cha machiritso ndi kupangitsa odwala kuti akhale bwino. Koma machiritso ndi mamasulidwe ali ndi zolinga zina zosiyana ndi kungom' pangisa munthu kuti akhale bwino

KUWONETSERA CHIKHALIDWE CHA MULUNGU

Machiritso amaonetsera kuti Mulungu ndu wachisomo, wabwino, chifundo, ndi wokhudzidwa:

Yehova ndiye wacisomo, ndi wacifundo; Osakwiya msanga, ndi wa cifundo cacikuru. Yehova acitira cokoma onse; Ndi nsoni zokoma zace zigwera nchito zace zonse. (Masalmo 145:8-9)

Ndipo Yesu anagwidwa cifundo, natansa dzanja namkhudza iye, nanena naye, Ndifuna; khala wokonzedwa. (Marko 1:41)

KUMUKWEZA MULUNGU

Machiritso amabweretsa matamanda ndi kumukweza Mulungu:

Ndipo makamu ambiri a anthu anadza kwa Iye, ali nao opunduka miyendo, akhungu, osalankhula, opunduka ziwalo, ndi ena ambiri, nawakhazika pansu pa mapazi ace:

Ndipo Iye anawaciritsa; kotero kuti khamulo linazizwa, pakupenya osalankhula nalankhula, opunduka ziwalo nacira, ndi opunduka miyendo nayenda, ndi akhungu napenya, ndipo iwo analemekeza Mulungu wa Israyeli. Mbali yomukweza Mulungu imakhudzanso kumuopa Mulungu. Machiritso amabweretsa zimenezi: (Mateyu 15:30-31)

Koma m'mene anawaopsanso anawamasula, osapeza kanthu kakuwalanga, cifukwa ca anthu; pakuti onse analemekeza Mulungu cifukwa ca comwe cidacitika. (Macitidwe 4:21)

Koma panadza mantha pa anthu onse; ndipo 5 zozizwa ndi zizindikilo zambiri zinacitika ndi atumwi. (Macitidwe 2:43)

KUTSIMIKIZA KUTI YESU NDI MPULUMUTSI NDI WODZODZEDZA

Werengani Mateyu 8:14-17 mu Baibulo mwanu. Machiritso amene alembedwa apa akutsimikiza mau a mneneri:

...Iye yekha anatenga zofoka zanthu, nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:17)

Machiritso ndi mamasulidwe amatsimikidza kuyi Yesu ndi mpulumutsi. Kuchiritsidwa kwa olumala ndikukhulukidwa kwa machimo ake kunatsimikiza kuti Yesu ndi mpulumutsi komaso ngati mchiritso. (Luka 5:18-26).

Ngati sindicita nchito za Atate wanga, musakhulupirira Ine. Koma ngati ndicita, mungakhale simukhulupirira Ine, khulupirirani nchitozo; kuti mukadziwe ndi kuzindikira kuti Atate ali mwa Ine, ndi ine mwa Atate. (Yohane 10:37-38)

Ndipo zizindikilo zina zambiri Yesu anazicita pamaso pa akuphunzira ace, zimene sizinalembedwa m'buku ili; koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace. (Yohane 20:30-31)

KUTSIMIKIZIRA NTHENGA NDI UTHENGA

Werengani nkhani ya kachiritsidwe ka mwana wa mwamuna pa 1 Mafumu 17. Pamene mwanayu anachiritsidwa, mayi ake anati kwa mneneri Eliya:

... Ndizindikira tsopano kuti ndinu munthu wa Mulungu, ndi kuti mau a Yehova ali m'kamwa mwanuwo ngoona. (1 Mafumu 17:24)

Machiritso amatsimikiza uthenga ndi nthenga.

Cifukwa cace anakhala nthawi yaikuru nanenetsa zolimba mtima mwa Ambuye, amene anacitira umboni mau a cisomo cace, napatsa zizindikiro ndi zozizwa kuti zicitidwe ndi manja ao. (Macitidwe 14:3)

Baibulo limakamba kuti patachitika chozizwa chachikulu cha machiritso, adzitsogoreri a uzimu ndi andale...

... koma pakuona kulimbika mtima kwa Petro ndi Yohane, ndipo pozindikira kuti ndiwo anthu osaphunzira ndi opulukira, anazizwa ndipo anawazindikira, kuti adakhala pamodzi ndi Yesu. (Macitidwe 4:13)

KULIMBIKITSA KALANDIRIDWE KA UTHENGA WABWINO

Ndikosavuta kuwauza anthu za Uthenga Wabwino pamene achiritsidwa. Pali zitsanzo zambiri za izi mu buku la Machitidwe. Machiritso amatsekula makomo a Uthenga Wabwino wa chipulumutso kuti ugawidwe, kudzadzidwa kwa Mzimu Woyera, ndikukula kwa mpingo. Onani Machitidwe 2:42-47 ndi 5:14 pa zitsanzo.

Ngakhale machiritso amalimbikitsa kuti Uthenga Wabwino ulandiridwe, nthawi zonse kumbukirani kuti samalowa mmalo mwakulalikira Uthenga Wabwino wachipulumutso. Mau akuyenera kulalikidwa motsatana ndikuonetsera mphamvu kupyolera kuchiritsa ndikumasula ndicholinga chobweretsa anthu muubwere wabwino ndi Mulungu. Nthawi zonse kumbukirani kuti ndi mau amene amalenga chikhulupiriro chopulumutsa, kuchiritsa, ndi kumasulu.

Machiritso ndi chida champhamvu polalikira Uthenga. Muzolembedwa zokhudza machiritso m'malemba:

1. Malo okwana nkhumu kasanu ndi kawiri, machiritso anachitika munthawi yomwe uthenga umkalalikidwa:

Mateyu 4:24; 8:16; 9:2-8; 9:32-33

Marko 1:23-28; 9:14-27; 10:46-52

Luka 8:42-48; 13:10-13, 16; 14:1-4; 17:11-19

Yohane 4:28-30; 5:1-9, 14; 9:1-7

Machitidwe 3:1-10; 8:5-8; 14:8-10

2. Malo okwana khumi asanu ndi limodzi, machiritso anali zotsatira za kulakira Uthenga Wabwino:

Mateyu 9:2-8; 9:32-33; 12:9-13

Marko 1:23-28; 5:1-13, 18-20; 7:32-37; 9:14-27

Luka 5:12-14; 13:10-13, 16; 17:11-19

Yohane 4:28-30; 9:1-7

Mchitidwe 3:1-8; 8:5-8; 9:32-35; 14:8-10

3. Mumalo makumi awiri ndi limodzi mwa malo makumi awiri asanu ndi limodzi, kunali kulalikira Uthenga kapena zotsatira.

KUKHAZIKITSA UFUMU WA MULUNGU

Machiritso ndi mamasulidweomwe anachitika ndi Yesu ndi ophunzira Ake anani gawo loyamba lokhazikitsa Ufumu wa Mulungu:

Ndipo ciritsani odwala ali mamwemonimunene nao, Ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu. Koma ku mudzi uli wonse mukalowako. (Luka 10:9)

Ndipo Yesu anayendayenda m'Galileya monse, analikuphunzitsa m' masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumu, naciritsa nthenda zonse ndi kudwala konse mwa anthu. (Mateyu 4:23)

Pamene mukutumikira machiritso, kumbukirani kuti ufumu sunakhazikitsidwe mwanthunthu. Ufumu ukazakhazikitsidwa mwanthunthu matenda ndi imfa sizizakhalaposo. Iziso zirichomodzimodzi ndi matenda. Kudwala ndi chilango chamachimo anthu akale. Tikhoza kuwomboledwa kumphamvu yake panakali pano, koma osati kupezeka kwake mpakana mtsogolo.

KUWONETSERA CHILANGO KWA MDANI

Pamene mukusanjika manja pa wodwala makhala mukulengeza kuti kalonga wa dziko lino waweruzidwa ndipo mphamvu ya madwale ndi matenda yaonongedwa (Yohane 16:11). Kumbukirani kuti ndi mphamvu ya matenda yomwe yawonongedwa, osati kupezeka kwake. Tizaomboledwa kukupezeka kwake pamene tizakhala kwamphumphu mu Ufumu wa Mulungu.

KUDZUTSA ATSOGOLERI AUZIMU

Machiritso akhala akugwiritsidwa ntchito podzutsa atsogoleri auzimu, Paulo anayitanidwa kuti akhale mtumwi wa Uthenga Wabwino panthawi yakuchizidwa kwake (Machitidwe 9).

AMABWERETSA CHIMWEMWE CHACHIKULU

Werengani Machitidwe 8:5-25. Ndime imeneyi ikufotokoza za chimwemwe chachikulu chomwe chinabwera kwa anthu ndi madera omwe machiritso ndi mamasulidwe anatumikiridwa.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiritso.

2. Pophatikidzira ku ungiro wa thupi, kodi zolinga zina 9 za machiritso zomwe zakambidwa mu phuzirori ndi ziti?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

Mulungu ali ndi zolinga zina zamachiritso ano pamwamba pa ungwiro wathupi. Pakumvetsetsa zolingazi zikupangitsani kuti mudzipempha machiritso ndi kulimbika mtima, podzindikira kuti ndi chifuniro cha Mulungu. Ganizirani momwe machiritso anu anga:

Onetsere chikhalidwe cha Mulungu:

Kwezere Mulungu:

Tsimiki dzire kuti Yesu ndi Mpulumutsi ndi wodzodzedwa:

Angakutsimikizireni inu ngati mtumiki ndi uthenga womwe mukuphunzitsa:

Angalimbikitsire olandira Uthenga Wabwino:

Ungakhadzikitsire Ufumu wa Mulungu:

Ungawonetsere chiweluzo pa mdani:

Momwe angabweretsere chimwemwe chachikulu:

CHAPUTALA 10

MPHATSO YA MACHIRITSO

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezo la machiritso.
- Kudzindikira Mzimu Woyera ngati mbali ya Utatu wa Mulungu
- Kulemba mwachidule utumiki wa Mzimu Woyera
- Kutanthauzira “mphatso za uzimu”
- Kutanthauzira “mphatso ya machiritso.”
- Kulemba mphatso za uzimu zomwe zimathandidzira mphatso ya machiritso.
- Kudzindikira yemwe akuyenera kutengapo gawo pa utumiki wa machiritso.

LONJEZO LA MACHIRITSO

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa... ndi kwa wina mphatso za machiritso, mwa Mzimu mmodziyo. (1 Akorinto 12:7-9)

CHIYAMBI

Baibulo limapereka okhulupirira onse kuti atengepo gawo pa utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe, koma Mawu amatsikimidziranso kuti pali mphatso zomwe zimaperkedwa kwa okhulupirira ena ndi Mzimu Woyera. Phunziro iri likuonetsera Mzimu Woyera ngati mbali ya Utatu wa Mulungu, kukamba machidule utumiki Wake, kutanthauzira mphatso zauzimu, ndi kukamba mphatso ya machiritso ndi mphatso zina zothandidzira.

MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ndi mbali ya Utatu wa Mulungu omwe uli Mulungu Atate, Mwana Yesu Khristu, ndi Mzimu Woyera. Chikhalidwe cha pautatu wa Mulungu chikuonetseredwa mu mdime zotsatirazi: Mateyu 3:16-17; Yohane 15:26; Aroma 8:2-3; 2 Akorinto 13:14; Aefeso 2:18; 1 Petro 4:14; ndi Machitidwe 2:33. Mzimu Woyera amapezeka paliponse (Masalimo 139:7). Amadziwa zonse (1 Akorinto 2:10-11). Ndiwamphamvu zonse (Masalimo 62:11). Ndiwamuyaya (Ahebri 9:14).

UTUMIKI WA MZIMU WOYERA

Mzimu Woyera ali ndi mautumiki ambiri. Nazo zimene Baibulo limanena za udindo Wake:

Chirengedwe: Anali ochitachita pakulengedwa kwa dziko.

Malembo: Amatumikira pakubvumbulutsa ndi kuuzira mpweya malembo ndi kupitiraza kutumikira kuunikira mitima yathu kuti timvetsetse Mawu.

Israyeli: Mzimu Woyera anabwera pa adzitsogoleri a Israeli, kuwatsogolera ku dziko lamalonjedzano, kudzadza malo awo amalambiro, ndipo adzabwera pa iwo mtsogolo panthawi ya matsautso.

Yesu: Yesu anabadwa, kudzodzedwa, kutsindikidzidwa, kutsogodzedwa, kupatsidwa mphamvu, kudzanidwa, kuperekedwa ku imfa, ndi kuukisidwa kwa akufa ndi Mzimu Woyera.

Ochimwa: Ochimwa amadzudzulidwa ndi kubweretsedwa ku Uthenda Wabwino ndi Mzimu Woyera.

Satana: Mphamvu ya Satana imakanidzidwa ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

Mpingo: Mzimu Woyera anapanga Mpingo, kulimbikitsa malambiro, kutsogolera mautumiki ake, kutsankha adzitsogoleri ake, kudzodza olalikira, kutsogolera maganizo ake, ndi kuwubatiza ndi mphamvu.

Okhulupirira: Mzimu Woyera amatsutsa okhulupirira za tchimo, kuyeretsa, kubatiza ndi mphamvu, kukhala nawo limodzi, kuwapatsa mphamvu, kumabweresa pamodzi, kuwapempherera, kuwatsogolera, kuonetsera chikondi, kutsandulizika ku chifaniziro cha Khritsu, kuonetsera choonadi, kuphunzitsa, kupereka chitsimikidzo cha chipulumutso, kupereka ufulu, kutonthoza, kupereka moyo, kulankhula ndi kapena kudzera mwa okhulupirira, kuonetsera mphamvu ya Mulungu, kulimbikitsa kulambira, kulimbikitsa kuchitira umboni, ndi kukulitsa zipatso ndi mphatso zauzimu. Ntchito yofunikira kwambiri ya Mzimu Woyera mu moyo wa okhulupirira ndi Mpingo yomwe imakhuzana ndi machiritso ndi mamasulidwe ndi kupereka mphatso za uzimu.

MPHATSO ZA MZIMU WOYERA

Mphatso zauzimu ndi kuthekera kwa uzimu koperekedwa ndi Mzimu Woyera kwa okhulupirira kuti akautimikire ngati mbali ya Thupi la Khristu. Pali kutsiyana pakati pa “mpatso ya Mzimu Woyera” ndi “mphatso za Mzimu Woyera.” “Mphatso ya Mzimu Woyera” inaperekedwa pa tsiku la Pentekoste yomwe inalembedwa pa Machitidwe 2. “Mphatso za Mzimu Woyera” ndi kuthekera kwa uzimu koperekedwa kwa omwe alandira mphatso ya Mzimu Woyera. Mphatsozi zimathandidza okhulupirira kutumikira mwamphamvu mu Thupi la Khristu ndi kwa osakhulupirira.

Mphatso ya uzimu si luso kapena kuthekera kwa ku thupi. Ndi kuthekera kwa uzimu koperekedwa ndi Mzimu Woyera. Munthu sagwiritsa ntchito, kukuza, kapena kukhala ndi mphatso za uzimu paiye yekha. Mphatsozi ndi kuthekera kwa uzimu koperekedwa ndi kugwiritsidwa ntchito kudzera mwa munthu ndi Mzimu Woyera. Mutha kuwerenga za mphatso za uzimu mu mdime zotsatirazi

-Aroma 12:1-8

-1 Akorinto 12:1-31

-Aefeso 4:1-16

-1 Petro 4:7-11

Pamene mukadzindikire mumavesiwa, pali mphatso zauzimu zambiri zomwe zaperekedwa ku Mpingo. Phunzirori likukamba za mphatso ya machiritso.

MPHATSO ZA MACHIRITSO

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao.

Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa... ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo. (1 Akorinto 12:7-9)

Okhulupirira wa mphatso yamachiritso ali ndi kuthekera kutulutsa mphamvu ya Mulungu yobwezeretsa nthanzi pamwamba pogwiritsa njira za kuthupi. Anthu onse okhulupirira anatomidwa kukapempherera odwala, koma okhulupirira yemwe ali ndi mphatso yamachiritso amagwiritsidwa mwapaderadera ndi mowirikidza ndi Mulungu mu iyi ya utumiki.

Pali mitundu yosinasiyana ya mphatso zamachiritso. Kuli mitundu yosiyana siyana ya matenda ndi mphatso zosiyana zamachiritso kuti akachiritse matendawo. Lingalilani njira zambiri zomwe Mulungu amagwiritsira ntchito pofuna kupulumutsa munthu. Kodi sangagwiritseso njira zambiri kuti abweretse machiritso? Njira kapena mphatso mwazokha sizimachiritsa kuposa kupulumutsa. Ndi njira zimene mphamvu ya Mulungu zimawonetsedwera.

Mu Baibulo timapeza kuti machiritso anachitika po:

1. Kusanjika manja: Mtumiki kukhudza odwala.
2. Anthu kumukhudza mtumiki.
3. Kuyakhula mau kuchokera patali.
4. Kuyakhula mau pamaso pa odwala.
5. Kuchita naye wodwala maso ndi maso.
6. Kuchiritsa chifukwa chamapembedzero a anthu ena.
7. Kupemphera.
8. Ntchito ya chikhulupiriro: machiritso amene amachitika kudzera mu mphamvu ya chikhulupiriro chomwe wodwala alinacho.
9. Mitundu yosiyanasiyana yachikhulupiriro yomwe ikugwira ntchito.
 - Chikhulupiriro cha yemwe akutumikira.
 - Chikhulupiriro cha munthu yemwe akufuna machiritso.
 - Chikhulupiriro cha abwenzi.
 - Chikhulupiriro cha abale.
10. Anagwiritsa ntchito zinthu zosiyanasiyana. Panalibe choyera mwachokha, koma zinagwira ntchito kukhala pamalo okumanira.
 - Mate.
 - Thope.
 - Nsalu zopemphereredwa.
 - Masamba a mkuyu.
 - Mphonje ya chovala cha mtumiki.
 - Chithuzithuzi cha mtumiki.

- Mafuta.
- Zaka makutu.
- Madzi.
- Kukhudza.

11. Zozizwa zapaderadera. Mulungu amadzodza anthu ena ndi chikhulupiriro chamachiritso mwapaderadera (Monga mtumwi Paulo). Mwachitsanzo, Mulungu amagwiritsa ntchito anthu ena kuti atumikire mwapaderadera kwa amene akudwala khansa, ndi ena otero. Izi sizikutanthauza kuti tisatumikire madera onse ofunikira machiritso, chifukwa tinalamulidwa kuti tikachiritse odwala onse.

MPHATSO ZOKHUDZANA NDI MACHIRITSO

Mphatso zonse za uzimu ndizofunikira kwambiri mu Thupi la Khristu, koma nazo zina mwa mphatso zomwe zimathandidzira mphatso ya machiritso.

Kuphunzitsa ndi Kulimbikitsa: Kuchokera pa Mawu, zimakuza chikhulupiriro cha machiritso.

Chinenero, Malilime amitundu mitundu, Mamasulidwe a malilime: Amabweretsa mawu kuchokera kwa Mulungu okhudzana ndi matenda ndi/kapena machiritso.

Chidzindikiro cha Mizimu: Imadzindikiritse ngati machiritso kapena mamasulidwe akufunika ndi chidziwitso cha mzimu omwe ukugwira ntchito.

Mphatso ya Chikhulupiriro: Imabweretsa kulimbika mtima kwapaderadera pa chidziwitso chomwe chabweretsedwa ndi kudzindikira kwa mizimu ndi kupemphera pemphero la chikhulupiriro.

Mawu a Chidziwitso: Imapereka chidziwitso cha gwero la matenda. Imathandidza kwambiri akakhala matenda amalingaliro kapena matenda akuthupi akukhudzana ndi ziwanda. Imapereka chidziwitso pa matenda omwe akuyenera kulapidwa, mphamvu ya ziwano yomwe yatengapo mbari, ndi maganizidwe amene akuletinga machiritso.

Mawu a Nzeru: Amakuthandidzirani kuti mugwiritse ntchito chidziwitso chomwe Mulungu wapereka cha “mawu a nzeru” (malangizo) kwa munthu wodwala.

Mphatso ya Machitidwe a Mphamvu: Machiritso apompopompo ndi olenga, mwachitsanzo, kukula kwa miyendo. Ndi zinthu zoti kafotokozeredwe kakumunthu sikangachitike, chinthu choti sichikanatheka kuchitika mu njira zakuthupi. Mutha kuphunzira zambiri zokhudzana ndi mphatso za uzimu mu phunziro la Harvestine International Institute lotchedwa “*Utumikiwa Mizimu Woyera.*”

KUFUNA MPHATSO ZA UZIMU

Baibulo limaphunzitsa kuti okhulupirira wina ali yense ali ndi mphatso ya uzimu:

Monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a cisomo ca mitundu mitundu ca Mulungu. (1 Petro 4:10)

Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. kwa wina cikhulupiriro, mwa Mzimu yemweyo; ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo. (1 Akorinto 12:7,9)

Chifukwa okhulupirira wina aliyense ali ndi mphatso ya uzimu, tiri ndi udindo wodzndikira ndi kugwiritsa ntchito mphatso yathu. Baibulo likuta tikuyenera kusaka mphatso za uzimu.

...funitsitsani mphatso zoposa... (1 Akorinto 12:31)

Pamene mukupera kuti mukhale ndi mphatso za uzimu, mukumupempha Mulungu kuti akunze mphatso zomwe ziri kale mwa inu, poti okhulupirira onse ali ndi ulamuliro oyalika manja pa odwala kuti achiritsidwe. Yesu anachurukitsa zinthu zomwe analandira (Luka 5:22) ndipo Timoteo anawidzidwa kuti akoleze mphatso yomwe iri mwa iye (2 Timoteo 1:6).

UTUMIKI WA MPINGO

Okhulupirira onse anapatsidwa ntchito yokachiritsa odwala, ndipo ngakhale Mulungu amayenda mwa ena ndi mphatso zapaderadera za machiritso, okhulupirira onse akuyenera kutengapo mbali pa utumiki wa machiritso. Awa ndi omwe Baibulo limati azitengapo mbali pa utumiki wa machiritso:

-Azibusa (Adzitsogoleri a uzimu):	Ezakieli 34
-Akulu a mpingo/azitumiki:	Yakobo 5:14
-Okhulupirira wana aliyense:	Luka 16:15-18; Yakobo5:16
-Omwe ali ndi mphatso yamachiritso:	1 Akorinto 12:9
-Mpingo wonse-ukuyenera kukhala malo amachiritso:	Luka 14:16-24

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezo la machiristo.

2. Mzimu Woyera ndi ndani?

3. Lembani mwachidule zomwe mwaphunzira za utumiki wa Mzimu Woyera mu phuzniro ili.

4. Kodi “mphatso za uzimu” ndi chani?

5. Tanthauzirani “mphatso ya machiritso.”

6. Kodi mphatso za uzimu zomwe zimathandidzira mphatso ya machiritso ndi ziti?

7. Kodi yemwe akuyenera kutengapo gawo pa utumiki wa machiritso ndi ndani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Kodi mukumvutika kukhulupirira chozizwa pa nthanzi lani kapena la amene mukumutumikira? Mulungu anlenga dongosolo lachirengedwe, koma siwomangidwa ndi iyo. Chozizwa chimachitika pamene Mulungu wayenda mopitirira malire akutthupi. Kwenikweni, machiritso achozizwa ndi kubwenzeretsedwa ku ungwirro. Ndi matenda ndi kudzadzidwa ndi ziwanda kumene kuli kotsiyana ndi chifuniro changwiwo cha Mulungu. Ndipo, machiritso, mamasulidwe, ndi kubwedzeretsedwa ku chifuniro cha Mulungu. Mu zoono zenizeni, si zozizwa zomwe ziri zodabwitsa, koma kutsapezeka kwa zozizwitsa mu utumiki wathu.
2. Mu buku la Machitidwe, onani anthu osiyanasiyana omw Mulungu anawagwiritsa ntchito mu mphatso ya machiritso.

-Machitidwe 3:1-11:	Petro ndi Yohane (Atumwi)
-Machitidwe 5:15; 9:32-34	Petro (Mtumwi)
-Machitidwe 8:5-7:	Filipi (Mlaliki ndi otumikira)
-Machitidwe 9:17-18:	Ananiya (okhulupirira)
-Machitidwe 14:8-10; 28:7-9:	Paulo (mtumwi)

3. Mzimu Woyera ndiye opereka mphatso za uzimu. umu ndi mene mungalandirire ubazo wa Mzimu Woyera:

-Lapani ndi kubatizidwa:	Machitidwe 2:38
-Khulupirirani kuti ndi wanu:	Machitidwe 2:39
-Ukhumbeni:	Yohane 7:37-39
-Uvomerezeni ngati mphatso	Machitidwe 2:38
-Ziperekeni kwa Mulungu	Yesaya 28:11; Machitidwe 2:4
-Pemphani mapemphero a okhulupirira ena	Machitidwe 2,4,10

4. Onaninso ndime za mphatso zamachiritso:

-Aroma 12:1-8 -1 Akorinto 12:1-31 -Aefeso 4:1-16 -1 Petro 4:7-11

Kodi mwdzindikira mphatso yanu (zanu)? _____ Ngai ziri choncho, kodi mukugwiritsa ntchito kutumikira ena? _____ Ngati simukugwiritsa ntchito mphatso yanu, kodi mungayambe bwanji kuyigwiritsa ntchito?

5. Pa zoonjezera za maphunziro a Mzimu Woyera ndi mphatso za uzimu, pezani phunziro la Harvestine International Network lotchedwa “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*”

GAWO LACHINAYI

KUGONJETA ZONTCHINGA

Kukhondo yakuthupi pamene mukumenyana ndi thupi ndi kufuna kukhala wamphumphu monga mmene Mulungu afunira, muzakumana ndizotchinga zikuzikulu zomwe mkuphatikizapo:

- CHIKHALIDWE CHA ANTHU.
- MINGA M'THUPI.
- MAFUNSO OPANDA MAYANKHO.

Mu gawo lino muzikozekeretsa nokha ndi Mau a Mulungu kuti mukumane ndi kugonjrtsa zotchinga zimenezi.

CHAPUTALA 11

CHIKHALIDWE CHA ANTHU

ZOLINGA:

Poliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa izi:

- Kulemba lonjezana lamachiritso osawonera.
- Kuyakhapo pazikhalidwe za anthu zotsatirazi pazokhudza machiritso.
- Machiritso ndi zozizwa sizamasiku ano.
- Nchifukwa chani akufa onse sanaukitsidwe?
- Nchifukwa chani akristu amamwalira?
- Makhwala atsopano akupangitsa kuti machiritso akumwamba akhale opanda ntchito.
- Machiritso akumwamba amaphunzirsidwa ndi mipingo yongenga.
- Thupi ndilofunika kwambiri kuposera moyo.
- Mukudwala chifukwa cha tchimo lanu.
- Ndichifuniro cha Mulungu kuti inu muzidwala.
- Ichi chizuzo cha olungama.
- Machiritso akumwamba ndiosowa.
- Kudwala kwaanu ndi nthanda wanu.

LONJEZANO LAMACHIRITSO:

Moyo wanga umamatika ndi pfumbi; Mundipatse moyo monga mwa mau anu. Ndinafotokozera njira zanga, ndipo munandiyankha: Mundiphunzitse malemba anu. Mundizindikiritse njira ya malangizo anu; Kuti ndilingalire zodabwiza zanu. Moyo wanga wasungunuka ndi cisoni: Mundilimbitse monga mwa mau anu. (Masalmo 119:25-28)

MAU OTSOGOLERA

Chikhalidwe cha anthu ndi zikhulupiriro, malamulo, ndi ndondomeko za munthu zomwe zimatchinga ntchito ya Mau a Mulungu. Yesu anawauza atsogoleri achipembedzo munthawi Yake:

...Ndipo inu mupeputsa mau a Mulungu cifukwa ca miyambo yanu. (Mateyu 15:6)

Ngati chikhulupiriro chimabwera chifukwa chakumva Mau a Mulungu, ndekuti chikhoza kuchokaso pakumva ndi kulandira zikhalidwe za anthu zomwe zimawononga chikhulupiriro.

Phunziro lino likukamba zikhalidwe za anthu zokhudzana machiritso. Kuyakha kwa Baibulo ku chikhalidwe kwaperekedwadwaso popeza kukoza kwabwino kwacholakwika sikukhala chete, koma kulalika chowonadi cha Mau a Mulungu. Pamene tikuchotsa zikhalidwe ndi zotchinga

zokhudzana ndi machiritso timachotsa zomwe zikutchinga machiritso akumwamba kuti asachitike.

Olemba Masalimo Davide anawonetsera kuti ngakhale kale anadalira njira zake zake kona tsopano akukhumba kuphunzirano njira za Mulungu:

Moyo wanga umamatika ndi pfumbi; Mundipatse moyo monga mwa mau anu. Ndinafotokozerana njira zanga, ndipo munandiyankha: Mundiphunzitse malemba anu. Mundizindikiritse njira ya malangizo anu; Kuti ndilingalire zodabwiza zanu. Moyo wanga wasungunuka ndi cisoni: Mundilimbitse monga mwa mau anu. (Masalmo 119:25-28)

Davide anasithanitsa chikhalidwe ndi Mau a Mulungu, ndipo pakuchita choncho, moyo wake unatsitsimuka (kuchiritsidwa ndi kubwezeretsedwa).

Izi ndi zina mwa zikhalidwe za anthu zokhudzana ndi machiritso:

“MACHIRITSO NDIZOZIZWA SIZAMASIKU ANO”

Anthu ena amati machiritso anali anthawi ya Baibulo yokha kapena mtsogolo pamene Yesu azabweraso.

KUYAKHA KWANTHU:

Mulungu anati:

... pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)

“Ine ndine” akukamba za pano. Ndetingasithe bwanji kukhala “Nalipo” kale kapena “Ndizakhalapo” mtsogolo? Baibulo limaphunzitsa kuti Mulungu samasitha:

Mphatso iri yonse yabwino, ndi cininkho ciri conse cangwiro zicokera Kumwamba, zotsika kwa Atate wa mauniko, amene alibe cisanduliko, kapena mthunzi wa citembenukiro. (Yakobo 1:17)

Pakuti Ine Yehova sindisinthika... (Malaki 3:6)

Mulungu sanasithapo chiyambireni chanthawi:

Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse. (Ahebri 13:8)

Ngati tsiku lazozizwa linali lakale, ndekutiso ziri chimodzimidzi ndi tsiku lachipulumutso, popeza palibe chozizwa chachikulu chopsa chipulumutso. Ngati machiritso ndi atsogolo pamene Yesu azizabweraso ku dziko lapansi, ndekuti utumiki wa aphunzitsi, abusa, ndie atsogoleri ena ukuyenera kukhalaso wanthawi yamtsogolo chifukwa mphatso ya machiritso ndi ndi mphatso ya uzimu monga mmene aliririso mautumikiwa.

Kuyakha kubwino kogwira moyo pazokamba zoti zozizwa sizamasiku ano zalembedwa pazomwe zinachitika. Ziripo zisanu ndi ziwiri “kuperekedwa” kapena “nthawi” imene Mulungu anachita ndi munthu munjira yapaderadera. Zimenezo ndi izi:

- Nyengo yopanda cholakwa Genesis 1:28
- Nyengo yachikumbumtima Genesis 3:23
- Nyengo ya ulamuliro wa munthu Genesis 8:20
- Nyengo yamalonjezano Genesis 12:1
- Nyengo yachilamulo Eksodo 19:8
- Nyengo yachisomo Yohane 1:17
- Nyengo ya Ufumu Aefeso 1:10

Kubwera kwa Yesu kuzakhala chikhazikitso chomaliza cha nyengo ya Ufumu. Kumayambiriro anyengo imeneyi, Yesu anachita zozizwa ndi kuchiritsa:

Ndipo anayankha, nati kwa iwo, Mukani, muuze Yohane zimene mwazona, nimwazimva; anthu akhungu alandira kuona kwao, opunduka miyendo ayenda, akhate akonzedwa, ogontha akumva, akufa aukitsidwa, kwa aumphawi ulalikidwa Uthenga Wabwino. (Luka 7:22)

Buku la Machitidwe linalimba zozizwa ndi machiritso mu mpingo woyamba pamene nyengo ya Ufumu imapitirirabe. Zolembedwa zatsopano za mbiri ya mpingo zimavomerezaso kuchitika kwa machiritso ndi zozizwa.

“NCHIFUKWA CHANI AKUFA ONSE SANAUKITSIDWE?”

Anthu ena amafunsa, “Ngati machiritso ndi alero, nchifukwa chani okhulupirira samamka kuzulira kumakadzutsa onse amene anadwala mkumwalira?”

KUYAKHA KWANTHU:

Kudzutsa akufa sinali mbali ya Kutumidwa Kwakukulu komwe konaperekedwa ku Mpingo. Kunalamulidwa kwa ophunzira pamene anatumidwa koyambirira kukalalikira kuti akalengeze Ufumu. Kuukitsa akufa chinali “chipatso choyamba” cha chiukitsa cha Yesu chomwe chimayembekezereka kubwera.

“NCHIFUKWA CHANI AKRISTU AMAMWALIRA”

Pamene tiri pa mutu wa imfa, ena amanena kuti ngati machiritso akumwamba amagwiradi ntchito, ndesipanakhala kristu aliyense anakamwalira.

KUYAKHA KWANTHU:

Kuyakhula uku sikunanenedwe ndi Malemba. Baibulo limapereka nthanzi lakumwanba mkatikati mwa nthawi ya moyo. Ngakhale imfa ya Yesu Khristu inatigulira chiwombolo ku imfa, thupi iri la nyama lizafa kumapeto kwake pokhapokha ngati Yesu atabwera nsanga ndikuchitika mkwatulo. Baibulo lomwero limaphunzitsa machiritso limaperekeso malire anthawi yomwe munthu atakhalire ndi moyo.

Masiku a zaka zathu ndiwo zaka makumi asanu ndi awiri, Kapena tikakhala nayo mphamvudi zaka makumi asanu ndi atatu... (Masalmo 90:10)

**Ndipo popeza 8 kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo 9 atafa, ciweruziro.
(Ahebri 9:27)**

**“MAKHWALA ATSOPANO AKUCHITITSA MACHIRITSO AKUMWAMBA KUTI
AKHALE OSAFUNIKIRA”**

Chikhalidwe chimati: “Kunalibe chithandizo chamakhwala chodaliririka mu nthawi ya Yesu. Kona tsopano kuti pano nthandizo liripo, ndetikuyembekezera kuti tiyambeno kugwiritsa ntchito izi mmalo mupepera kwa Mulungu kufuna machiritso.”

KUYAKHA KWANTHU:

Kuyambira kalekale mu 400 B.C, kunali njira yochiritsira kudzera makhwala. Munthu otchedwa Hippocrates (460-370 B.C), tate wamakhwala, anakoza ukadaulo wamakhwala apamwamba kwambiri. Wina mwaukadaulo wake ukugwiritsidwabe ntchito lero. Greece, Aigupto, ndi Roma anali ndi akadaulo azamakhwala mu nthawi ya Yesu.

Machiritso akumwamba alibe ndikuchita kwinkulikonse kaya kuyenera kaya kusayenera kwa makhwala aza sayasi. Ndi mdalitso omwe unaperekedwa pa imfa ya Yesu. Mphatso iriyonse yabwino imachokera kwa Mulungu, nde mkovomerezeka kugwiritsa ntchito makhwala amene ali omvemerezeka. Kumbukirani, makhwala simulowa mmalo wa pangano lamalonjezano la machiritso.

“MACHIRITSO AKUMWAMBA AMAPHUNZITSIDWA NDI MIPINGYONYENGA.”

Chikhalidwe chimati: “Machiritso akumwamba amaphunzidwa ndi mipingo yonyenga.”

KUYAKHA KWANTHU:

Wesley, Luther, ndi Zinzendorf, atsogoleri amipingo ya Methodist, Lutheran, ndi Moravian, onsewa anaphunzitsapo za machiritso akumwamba. Onse amene amaphunzitsa izi lero, pamodzi ndi mphamvu yopulumutsa ya mwazi wa Yesu Khristu ndi Umulungu Wake, ndiosamvomerezeka kuposa atsogolori amenewa.

Mipingo ina yonyenga imaphunzitsa machiritso, koma osati machiritso a Baibulo. Ndi “zaganizo” malingaliro apazithu chabe. Satana ndi onyenga ndi otsazira chabe. Sitichotsa machiritso akumwamba chifukwa ananyenga ndikuchiza kupyolera mu mphamvu zoipa.

Satana wanyenga anthu ambiri kuti akhulupirire kuti kukasambitsidwa mu mtsinje wa Ganges ku India ndekuti ayeretsedwa kumachimo. Kodi timaleka kulalikira chipulumutso chifukwa hakuti satana wakopera izi? Kodi inu maleka kukhulupirira akadaulo amakhwala chifukwa pali ena ochepa amene ali achinyengo? Choonadi nchakuti satana amakopera machiritso akumwamba ndi chizindikiro chakuti pali machiritso eni eni akumwamba.

“CHIDWI CHIMAIKIDWA PA THUPI KUSIYANA NDI MOYO”

Chikhalidwe chimati: “Machiritso akumwamba amaika chidwi kwambiri pa thupi okusiyana ndi moyo.”

KUYAKHA KWANTHU:

Ena amakhulupirira mu utumiki wamachiritso ukupezeka mu gulu limeneri, koma izi siziri mundondomeko yamachiritso ya Baibulo. Machiritso a Baibulo amathana ndi munthu yese wamphumphu, thupi, moyo ndi mzimu.

Machiritso si Uthenga Wabwino pawokha, ndi mbali imodzi ya Uthenga Wabwino wa Khristu. Usalalikidwe pawokha popanda uthenga wachipulumutso cha moyo wochimwa kwa amuna ndi akazi.

“MUKUDWALA CHIFUKWA CHA TCHIMO LANU”

Kunena kumodzi komwe kumanenedwa mkwakuti “Mukudwala chifukwa munachimwa kapena muli tchimo mmoyo mwanu.”

KUYAKHA KWANTHU:

Takamba kale izi pa phunziro lokhudzana ndi chiyamba komaso komwe kumachokera madwale mumachaputala 5 ndi 6. Mukumbukira kuti pamene matenda mdziko muno chifukwa cha tchimo, munthu sikuti amadwala chifukwa cha tchimo la munthu.

“NDI CHIFUNIRO CHA MULUNGU KUTI INU MUZIDWALA”

“Ndi chifuniro cha Mulungu kwa inu kuti muzidwala. Zimatengera ulemerero kwa Iye.”
Munayamba mwavako kuyakhula kumeneku?

KUYAKHA KWANTHU:

Ambiri samafunsa ngati Mulungu angathe kuchiritisa kapena ayi, koma ngati ali wofuna. Baibulo limanena kuti ife tiwopanda nzeru ngati sitimvetsetsa chifuniro cha Mulungu:

**Cifukwa cace musakhale opusa, koma dziwitsani cifuniro ca Ambuye nciani.
(Aefeso 5:17)**

Kudziwa chifuniro cha Mulungu pokhudzana ndi matenda kumapereka theka yachonde yomwe chikhulupiriro chingakulepo. Pemphero lachikhulupiriro ndi pemphero lokhalo limene limachita kuposa kutenga machiritso kwa odwala. Silingapemphereredwe pokhapokha mutazindikira ngati chiri chifuniro cha Mulungu kuti achilitse. Nthawi zina Mulungu amalola matenda kuti abwere kwa okhulupirira, koma nthawi zonse kumbukirani kuti satana ndi gwero lake. Chitsanzo cha Yobu chimawonetsera izi bwino (Yobu 1-2)

Mulungu sanafuna okhulupirira kuti okhulupirira azidwala. Amakhala akudziwa zachiwembu cha satana ndipo Amagwiritsa ntchito zinthu zonse (ngakhale zoyipa) kuti zigwire ntchito limodzi kukuchitirani inu ubwino. Ichi nchifukwa chake ngakhale pa nthawi yamatenda muthabe kukhala chifupi ndi Mulungu. Mulungu nthawi zonse amafuna kuti atulutse chabwino muchoipa. Anagwiritsa ntchito zotsatira za imfa pobweretsa imfa ya Yesu. Mulungu sichiyambi cha matenda amene ali mmoyo mwa okhulupirira, koma Mulungu amatenga chinthu chimene satana

amafuna kuchigwiritsa ntchito muyipa ndi kuchigwiritsa ntchito kuti chikwaniritse chipambano cha uzimu pamene mukudutsa muziwembu.

Paulo poyamba analalikira ku Galatiya koma kenako anasitha zokozero zake chifukwa chakudwala (Agalatiya 4:13-15). Kudwala kwa Trofimo kunamuletsa iye kupita ku Roma ndi Paulo (2 Timoteo 4:20). Kudwala kunagwiritsidwa ntchito ngati njira yopewera tchimo mu Genesis 12 ndi 20. Ngakahale zitsanzosi zikuwonetsera mmene Mulungu amagwiritsira izi ntchito, kumbukirani kuti...

Pakuti samasautsa dala, ngakhale kumvetsa ana a anthu cisoni. (Maliro 3:33)

Matenda pawokha samapanga oyera mtima amaene amamukweza Mulungu. Akhoza kutulutsa kudandaula kowawidwa mtima. Kusakhulupirira anthu. Ndi Mau amene amayeretsa ndi kubweretsa kukula (Yohane 17:17). Ngakhale kuti ndizowona kuti mumalowa kwakuya pamene mukudwala, ndenkho funikaso kuti mudwale kuti mukule mu uzimu.

Mkofunika kukumbukira ichi: cholinga cha Mulungu pa okhulupirira nchakuti akhale ngati Yesu machitidwe. Zina zonse, kuphatikizapo matenda ndi moyo wathazi, zimawonetsera ubwino umene ulipo pokhudzana ndi cholinga chakumwamba (Aroma 8:28-29).

Yesu anati, “Ngati wandiwona Ine, waonaso Atate.” Ananena izi chifukwa Anachita ntchito ndi chifuniro cha Atate (Yohane 14:9). Ngati madabwa ngati Mulungu akufuna kapena ayi kukuchiritsani, mukuyenera kungoyang’ana pamachitachita a Atate anthu.

Yesu anatiphunzitsa ife kupemphera “Kufuna kwanu kuchitidwe pansu pano, mongaso choncho kumwamba.” Palibe nthenda ndi madwale Kumwamba, nde tikhoza kupephera molimba mtima potsutana nawo pansu pano pozindikira kuti sichifuniro Chake. Yesu sanapemphere “chiritsani ngati kuli kufuna Kwanu, Mulungu.” Nthawi yokhayo imene Anapemphera “Ngati chili chifuniro Chanu” zinali zokhudzana ndi kuzipereka Kwake ku malingaliro a Mulungu pa Moyo Wake—osati machiritso. “Ngati chingakhale chifuniro chanu” chimawononga chikhulupiriro. Pamene linagwiritsidwa ntchito ndi wakhate amene samkamudziwa chifuniro cha Yesu pamachiritso, Yesu anamukonza kusakhulupirira kwake pomutsimikizira iye kuti, “Ndikuchiritsa.” Musamasandutse zowonadi za Mulungu kukhala chiyembekezo kapena mafunso.

Chifukwa choti wina sanachiritsidwe pompopompo kapena chifukwa chakuti wina wamwalira ndi “nthenda yotengera ku imfa” izi sizikutanthauza kuti sichifuniro cha Mulungu kuchiritsa. Timawona zinthu molingana ndi nthawi, pamene Mulungu amaziwona mwamuyaya. Mukuyenera kukumbukira kuti nthawi zina machitso amacheretsedwa. Ena ndi:

Kuchedwetsedwa ku nthawi yakuthupi: Kusabala kwa Sarai sikunachiritsidwe pompopompo. Yobu sanachiritsidwe pompopompo. Atate ake a Yohane m’batizi sanachiritsidwe kusayakhula kwawo kufira nthawi yoyikika itafika. Yesu anamupempherera kawiri munthu wakhungu amene anangolandira machiritso pang’ono pa nthawi yoyamba. Machiritso nthawi zina amachedwetsedwa kuti akabweretse ulemerero kwa Mulungu. Chitsanzo chabwino cha ichi ndi nkhani yakuukitsidwa kwa Lazaro.

Kuchedwetsedwa ku muyaya: Imfa ndichochitika chomwe chirimkatikati mwa zochitika zamuyaya mmoyo mwa wokhulupirira. Ngakhale “nthenda yofikits aku imfa” imamezedwa muchigonjetso chifukwa imfa kwa wokhulupirira ndi machiritso amphamvu. Pamene mulowa mkupezeka kwa Atate mapangidwa kukhala wagwiro ndipo simazuzikaso ndi tchimo kapena kudwala. Poyakhulapo za imfa, Paulo anati munakozezedwa chifukwa chazholinga chimenechi: “Kusowa ku thupi, ndikukakhala ndi Atate” (2 Akorinto 5:6-8)

Ngati simakhulupirira machiritso kuti ndi a anthu onse, nde mukuyenera kukhulupirira kuti machiritso amatsogozedwa ndi bvumbulutso lachindunji pa nthaw iriyonse kaya ndi chifuniro cha Mulungu kuchiza kapena ayi. Inu ndekuti mukuwerengera bvumbulutso lochokera kwa munthu osati Mau a Mulungu olembedwa. Simungakhale ndi maziko eni eni achikhulupiriro pokhapokha mutalandira bvumbulutso lapaderadera panthawi yodwala.

“ICHI NDI CHIZUZO KWA OKHULUPIRIRA”

Anthu ena amanena: “Zizuzo za anthu olungama ndi zochuluka. Ichi ndi chizuzo chimene mukuyenera kuchipirira chifukwa ndinu olungama.”

KUYAKHA KWANTHU:

Tanthauzo la mau akuti “kuzuzika” anagwiritsidwa ntchito mu Masalimo 34:19, komwe chikhalidwechi chinachokera, sizimatanthauza kuti kudwala. Amatanthauza kuyesedwa, zowawa, kuzuzidwa kapena mayesero. Ngakhale zitakhala kuti amkatanthauza matenda, chikumbutso cha vesi imeneyi nchakuti Atate akufuna kupulumutsa onse.

Mu Yakobo 5:13-16 imawonetsa kusiyana kwa kuzuzika ndi kudwala. Ngati mukumva zowawa ndi kuyesedwa, kuzuzidwa, ndi mayesero, mukuyenera kupemphera nokha (Yakobo 5:13). Ngakhale kuti mutha kuwapempha ena kuti apemphere nanu, sikuti aitanidwa kuti azapempherere mabvuto anu onse. Malemba akulamurani kuti mupemphere ngati mukumva zowawa chifukwa mukuyenera kuphunzira kukhala mgonjetsi popemphera panokha kupyolera mukuyesedwa. Panthawi yodwala, akulu ampingo akuyenera kuitanidwa kuzakupemphererani (Yakobo 5:14). Odwala akuyenera kupulumutsidwa (kukudwala kwawo kwakuthupi), kuukitsidwa (kubwereranso kwa mphamvu), ndikukhululukidwa kwamachimo awo (machiritso auzimu).

“MACHIRITSO AKUMWAMBA NDI OSOWA”

Ena amatsutsamachiritso akumwamba ndi osowa. Iwo amafunsa, “Nchifukwa chani kupangitsa chikhulupiro cha anthu kuti chidzuke mapeto ake mkuwakhumudwitsa?”

KUYAKHA KWANTHU:

Machiritso akumwamba siwosowa. Ma vesi amu Chipangano Chatsopano adzadza ndi nkhani zamachiritso ndi mamasulidwe. Zolembedwa za mbiri ya mpingo zinalembe zamachiritso akumwamba.

“KUDWALA KWANU NDI NTHANDA WANU”

“Kudwala kwanu ndi nthanda wanu. Mukuyenera kuphunzira kukhala nawo.” Munayamba mwavapo zokamaba izi?

KUYAKHA KWANTHU:

Kuyakhula kwakuti kudwala ndi “nthanda” wanu mkosavuta kuthana nako. “Nthanda” siamavuto, matenda, ndi chizuzo zomwe zimabwera painu popanda kusakha kwanu. Yesu ananena izi moveka bwino “kunyamula nthanda” ndi ntchito yongozipereka, osati chithu chimene malandira chifukwa chakuti mulibe kusakha. Yesu sananene kuti kudwala ndi imfa ndi nthanda ochokera kwa Mulungu. Ana zithenga izi ngati mdani. Ngati makhulupirira nthenda kuti ndi nthanda wanu, nde nchifukwa chani mafunafunaso chithandizo chamakhwala kuti muthana nayo?

MAYENSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lenjezano lamachiritso osawonera.

2. Lembani kayakhidwe ka zikhalidwe za anthu zotsatirazi:

Machiritso ndi zozizwa sizamasiku ano:

Nchifukwa chani akufa onse samaukitsidwa?

Ngati machiritso akumwamba amagwiradi ntchito, nchifukwa chiyani Akristu amamwaliraso?

Makhwala atsopano amapangitsa kuti machiritso akumwamba kuti akhale opanda pake:

Machiritso akumwamba amaphunzitsidwa ndi zipembedzo zonyenga:

Pamachiritso akumwamba, thupi ndilomwe limapatsidwa chidwi kwambiri kusiyana ndi moyo:

Mukudwala chifukwa cha tchimo lanu:

Ndi cholinga cha Mulungu kuti inu muzidwala:

Ichi ndi chizuzu cha olungama:

Machiritso akumwamba ndi osowa:

Matenda anu ndi nthanda wanu:

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwabukuli)

CHAPUTALA 12

MINGA M'THUPI

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano lamachiritso osawonera.
- Kufotokoza kuti minga imene inali m'thupi mwa Paoulo inachokera kuti.
- Kufotokoza mmene Baibulo limanenera kuti mingayo inali chani.
- Kufotokoza chifuka chomwe analolezedwera.
- Kunene zomwe inachita.
- Kulemba mwachidule mmene inawonetsedwera.
- Kufotokoza zotsatira za minga yomwe inali m'thupi mwa Paulo.

LONJEZANO LA MACHIRITSO LOTI TITENGE:

Ndipo Yehova adzakantha Aigupto kukantha ndi kuciritsa; ndipo iwo adzabwerera kwa Yehova, ndipo Iye adzapembedzedwa ndi iwo, nadzawaciritsa. (Yesaya 19:22)

CHIYAMBI

Muphunziro lapita lija mwaphunzira zikhalidwe zina za munthu zomwe zimabweretsa mavuto kwa okhulupirira amene akufuna machiritso ndi mamasuridwe. Phunziro lino likukhudzana chikhalidwe chimene chakhazikika pa minga yomwe inali m'thupi la Paulo yowe yafotokozedwa mu 2 Akorinto 12. Chifukwa nthawi zambiri pamakhala mtsutso ndiposo imakhudza kwambiri pa nkhani yamachiritso, ndetapereka phunziro lonseri kuzimenezi.

Anthu ambiri auzidwa kuti minga ya Paulo inali nthenda ndipo ngakhale anapemphera katatu kuti ichoke koma panalibe zotsatira, alonjezedwa kukakhala ndi “minga yawo m'thupi” lamatenda. Chikhalidwe chimati, “Kudwala ndi minga mthupi monga mmenri zinaliriso ndi Paulo ndipo mukuyenera kuphunzira kukhala nayo.”

“Minga m'thupi” chikhalidwe ndichotchinga chachikulu chomwe chimaletsa ambiri kuti asalandire machiritso. Yagwiritsidwa ntchito udyo poyesa kulongosola chifukwa chimene anthu samalandirira machiritso owoneka ndi maso ndipo ndichozikanila pakusowa nphamvu kwanthu. Pamene mukuyamba phunziro lino, muike pambali chinachirichonse chimene munaphunzidwa ndi munthu zokhudzana ndi nkhani imeneyi pamene tikufukula kuti tipeze chenicheni chimene Malemba amaphunzitsa.

MINGA M'THUPI LA PAULO

KODI INALI CHANI:

Baibulo limanena kuti “anali wantenga.” Pa Chigriki liwu loti “wanthenga” limawoneka kasanu ndi kawiri mu Chipangano Chatsopano. Linamasuliridwa kuti “mngelo” linagwiritsidwa ntchito nthawi kwa 181. Nthawi zonsezi limakamba za umunthu, osati matenda kapena madwale. “wanthenga” ndi munthu.

KODI INACHOKERA KUTI:

Baibulo limati inali wa nthenga wa satana.

NCHIFUKWA CHANI INALOLEZEDWA:

Paulo anati minga imeneyi inalolezedwa chifukwa chamabvumbulutso ochuluka amene analandira komanso chifukwa chachikhaliwe chake chozitamandira. Munthu wina aliyense asanayambe kunena kuti alindi minga thupi aziyamba kaye walingalira kuti kodi ndi mabvumbulutso ndi masomphenya angati amene alinawo. Kodi akukwanira kukhala ndi minga? Anthu ambiri amene amaganiza kuti alindiminga m'thupi mwawo amakhala kuti alibe bvumbulutso ndi masomphenya.

Minga inalinsu mbali imodzi yokwaniritsa uneneri. Pamene Paulo anatembenuka mtima, Mulungu anati:

...Pakuti Ine ndidzamuonetsa iye zinthu zambiri ayenera iye kuzimva kuwawa cifukwaca dzina langa. (Machitidwe 9:16)

ZOMWE INACHITA:

Minga inamuzuzwa Paulo. “Kuzuzwa” kumatanthauza kuti kmenya mobwereza, kabwerezabwereza. Mau oti “kuzuzwa” sakutanthauza kuti nyengo ya matenda yokhazikika koma kumenya mubwereza. Wanthenga anatomidwa kukamusautsa Paulo pofuna kuletsa Mau a Mulungu kuti asalalikidwe.

Mulungu sanalonjeze kuchotsa kuzuzika kwa okhulupirira, koma analonjeza kuchotsa matenda awokhulupirira. Malemba atichenjeza kawirikawiri kuti ngati tikhala mowonadi mtima tizalandira chizuzo ndimasautso, koma osati matenda.

KODI INAWONETSEREDWA BWANJI:

Nazo zina mwazitsanzo zomwe minga inatumphutsira chotsutsa kwa Paulo:

1. Ayuda anafuna kumupha Paulo atangotembenuka mtima kumene: Machitidwe 9:23
2. Paulo analetsedwa kukalumikizana ndi okhulupirira ena: Machitidwe 9:26-29
3. Anatsutsidwa ndi satana: Machitidwe 13:6-12
4. Anatsutsidwa ndi Ayuda pachimpwirikiti: Machitidwe 13:44-49
5. Anapirikitsidwa ku Antiokeya wa m'Pisidiya: Machitidwe 13:50
6. Anamenyedwa ndikupitikitsidwa ku Ikoniyo: Machitidwe 14:1-5

7. Anathawira ku Lustra ndi Derbe komwe anakagendedwa ndipo anasiyidwa ngati wamfa: Machitidwe 14:6-19
8. Anatsutsidwa kwambiri ndi abwenzi onyenga: Machitidwe 19:8
9. Anamenyedwa ndi kuikidwa mndende ku Filipi: Machitidwe 16:12-40
10. Anamenyedwa ndikupitikitsidwa ku Tesalonika: Machitidwe 17:1-10
11. Anamenyedwa ndikupirikitsidwa ku Bereya: Machitidwe 17:10-14
12. Anamenyedwa ku Korinto: Machitidwe 18:1-23
13. Anamenyedwa ku Aefeso: Machitidwe 19:23-31
14. Ayuda anampangira chiwembu chofuna kuchotsa moyo wake: Machitidwe 20:3
15. Anagwidwa ndi Ayuda, anazuzidwa, kuyesedwa kumabwalo amilandu kasanu, ndiposo anamva zina zowawa zambiri: 2 Akorinto 11:23-33

Palibe olo pamodzi, muzolembedwa zake, pamene Paulo anatchula matenda kukhala chizunzo chimene chinamuzuzwa. Mu 1 Akorinto 4:11, Paulo anawonetsera kuti lingaliro lake lakuzuzika silinali lokhazikika ngati matenda. Anati, “Kufikira nthawi yomwe yino timva njala, timva ludzu, tiri amaliseche, tikhomedwa, tiribe pokhazikika.” Paulo anadwalapo monga mmene zinalembedwera pa Agalatiya 4:13-16, koma iyi sinali minga yake chifukwa sinali nyengo yokhalitsa. Anati anadwala kumayambiriro kokha.

Ena amakhulupirira kuti minga ya Paulo inali diso lang’ala, koma maso ake anachiritsidwa ku khungu (Machitidwe 9:18). Kupitiriza kukhulupirira kuti anali ndi mvuto la maso zimatsutsana ndi mphamvu yamachiritso Amulungu. Komaso, kodi kunakakhala kwa bwino kunena mvuto la diso kuti linabwera chifukwa chowona ulemerero wa Mulungu kukhala wanthenga wa satana? Paulo mwini wake amatiuza kuti muchaka cha 60 A.D, pamene analemba kalata yake, panali patapita zaka 14 chilandirireni mabvumbulutso ochulukira amene anabweretsa minga thupimwake. Panali patatha zaka 12 chitembenekirireni mtima pamene anawona ulemerero wa Mulungu.

ZOTSATIRA ZAKE:

Paulo anayakhulapo za mazunzo ake kutanthauza kuti “amkasowa mphamvu, kufooka, kulephera kubweretsa zotsatira kupyolera mukuyesa yesa kwake.”

CHIMALIZIRO

Chimaliziro chokhudzana ndi minga ya Paulo ndichakuti sitingadziwe bwino bwino kuti mingayo inali chani, ngati munaphunzidwa kuti anali matenda kumbukira izi maganizo mwanu:

Minga ya Paulo inawonetsera mphamvu ya Mulungu mmoyo mwake. Anthu ena amagwiritsa ntchito “minga mthupi” pofuna kuzimbaitsa kumatenda. Akuyenera kuzindikira kuti zitsanzo za m’Baibulo zoterozo zinatsutsidwa ndi anzake omwe amayenda nawo mu utumiki. Minga sinamuletse kugwira ntchito mu Ufumu wa Mulungu kapena kuwonetsera mphamvu ya Mulungu kupyolera mwa iye.

MAYENSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani lonjezano la machiritso osawonera.

2. Kodi minga yomwe inali m'thupi la Paulo inachokera kuti?

3. Malingana ndi Baibulo, kodi minga m'thupi la Paulo inali chani?

4. Nchifukwa chani minga inalolezedwa kukhala m'thupi?

5. Kodi minga inachita chani kwa Paulo?

6. Kodi minga yomwe inali m'thupi mwa Paulo inawonetseredwa bwanji?

7. Kodi zotsatira zaminga m'thupi la Paulo zinali zotani?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Gwiritsani ntchito zimene mwaphunzira mu phunziro lino, mmene mungayakhire munthu amene akuyakhula kuti matenda awo anali “minga m’thupi mwawo” kuchokera kwa Mulungu?
-
-

2. Werengani lonjezano la machiritso:

...Iye adzapembedzedwa ndi iwo, nawachiritisa. (Yesaya 19:22)

“Kupembedza” kumatathauza kuti kupempha mowirikiza ndi molimbika be. Mulungu analonjeza kuchiritso onse amane amamupembedza Iye.

3. Ngakhale kuti minga ya Paulo sanali matenda, simungapephe mphamvu yomwe imaperekedwa kwa iye kaya pakuzuzika kwa mkati kapena kufooka kwa kuthupi pamene kukudikira kuchiritidwa kwa mphumphu.

Mulungu anamuyakha Paulo:

...Chisomo change chukukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m’ufooko. (2 Akorinto 12:9)

Kuyakha kwa Paulo kuzimenezi kunali...

...Chifukwa chake makamaka ndidzadzitamandira mokondweratu m’maufoko anga, kuti mphamvu ya Kristu ikakhale pa ine. Chifukwa chake ndisangalala m’maufoko. M’zowawa, m’zikakamizo, m’mazunzo, m’zipsinjiko, chifukwa cha Kristu; pakuti pamene ndifoka, pamenepo ndiri wamphamvu. (2 Akorinto 12:9-19)

4. Ganizirani zachithu chakuthupi kapena wina wake amene inu mukumutumikira machiritso:

Kodi chofooka chanu pano nchani?

Kodi mphamvu ya Mulungu ingawonetseredwe bwanji m’maufoko?

Pomene mudikira machiritso, pangachitike chani pofuna kubweretsa ulemerero kwa Mulungu? (Ngakhale onse amene agonekedwa pakama kapena ena ali pa njinga za anthu olumala akhoza kuchita chinachake. Mwachitsanzo, akhoza kukhala opemphedzera.)

5. Kodi mukukumana ndi chizuzo chakuthupi chochokera kwa satana kuphatikizapo pamavuto anu akuthupi?

Ndi mabvuto anji amene mukukumana nawo pano

Kodi ulemerero wa Mulungu ungawonetsedwe bwanji ndi nyengo zonsezi?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwabukuli)

CHAPUTALA 13

MAFUNSO OSAYAKHIDWA

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la Machiritso.
- Kupereka tanthauzo la “machitachita”
- Kufotokoza zotchinga zotsatirazi zimene zimatchinga machiritso.

Kusowa kwachiphunzitso

Kusakhulupirira

Kusowa chikhulupiriro

Kusowa mphamvu

Tchimo la inu eni losalapidwa

Kukana kuti mukozedwenso

Kusowa kopanga chiganizo ndi chikhumbokhumbo

Mavuto okhudzana ndi kupempha

Kusowa chipiriro

Kusamvera mundondomeko yamachiritso

Kusazindikira thupi la Kristu

Kusatulitsidwa kwa mizimu yoyipa

Kukopera ntchito ya Mulungu

Kumphanya malamulo achilengedwe cha Mulungu

Nthawi yoyikika yomwalira

- Kuyakha kuzotchinga.

LONJEZANO LAMACHIRITSO:

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (1992 Deuteronomo 29:29)

CHIYAMBI

Nchifukwa chani anthu ambiri samachiritsidwa? Nchifukwa chani ena amachiritsidwa pamene ena ayi? Nchifukwa chani akhristu amene ali osazikika kwambiri ndi achikunja amachiritsidwa pamene anthu amene ali owongoka komaso owona mtima ndi ozipereka sanalandirepo machiritso? Awa ndi ena amwamwa funso amene muzalandire pamene mwayamba kutumikira machiritso ndi mamasulidwe. Phunziro lino likukhudza machitamachita amene amasokoneza machiritso. Mchitidwe ndi chochitika chimene chamapangitsa kuti pakhale kusiyana kapena zotsatira zosiyana.

Mulungu analonjeza machiritso mmau Ake. Tikuyenera kukumbukira, kuti lonjezani lirironse la Mulungu lilindi malire mmene munthu angavomerere. Ichi nchifukwa chake nkoyenera kumvetsa bwino machitamachita omwe angaononge machiritso.

KUMVETSETSA NDI KUTHANA NDI MACHITACHITA

Machitachita mu utumiki wa machiritso ndi zifukwa zomwe anthu ena amachiritsidwira pamen ena ayi. Musanayambe phunziro ili, mkofunika kukumbukira kuti simuzakhala ndi mayankho afunso lilironse lomwe muzakumane nalo pa machiritso ndi mamasulidwe.

Ndichikhalidwe cha munthu chofuna kumvetsetsa chilichonse. Yeselo loyamba linakhazikika pa nkhani imeneyi. Khumbokhumbo lofuna kudziwa zinthu zonse limachokera kuukira pokhala ndi mafunso opanda mayankho. Mvuto limeneri lomwe munthu alinalo ndilomwe mukuyenera kuligonjetsa kuti mukakwanitse kutumikira machiritso ndimamasulidwe mwapindula. Baibulo limaulula mwamachitachita ena omwe amasokoneza machiritso ndi mamasulidwe, koma simudzakhala ndi mayankho pamafunso onse. Ngati mutero, simuzafunanso Mulungu kapena chikhulupiriro. Baibulo lilichindunji kuti zinthu zina ndizoululika kwa ife, pamene zina ayi:

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)

Mumachiritso ndimamasulidwe, mukuyenera kuphunzira kuyika pambali mafunso opanda mayankho, ndikusiyira Mulungu zinthu zonse zachinsisi.

Machiritso ndi mamasulidwe zirimbali ya Uthenga Wabwino monga ngati mmene chiririnso chipulumutso. Pamene mukutumikira machiritso ndi mamasulidwe ndipo ena sanalandire, muzayedwe kuti mungosiya. Koma lingalilani funso ili: Kodi masiya kulalikira chipulumutso chifukwa aliyense wamva Uthenga sanapulumsidwe? Nde nchifukwa chani mathamangira kuleka kutumikira machiritso ndimamasulidwe chifukwa aliyense sanalandire? Nchifukwa chake nthawi zambiri mmachiritso ndi mamasulidwe, kunyada kumalowapo. Timachita manyazi pomwe tapepherera munthu amene akudwala mowoneka ndipo sanachiritsidwe. Ena amatha kuwona chifukwa ndizakunja. Ngati wina avomera chipulumutso koma sanapulumsidwe, anthu sangawone chifukwa ndizamkati. Kunyada kwanthu kumakhudzidwa ndizomwe anthu amawona kunja.

Simuzakhala ndi mayankho azochitika zonse zomwe zimasokoneza machiritso monga ngatinso zochitika zina zomwe zimasokoneza chipulumutso. Ena amapulumsidwa, ena ayi. Ena amachiritsidwa, ena ayi.

Baibulo limaulula mwa zina mwazochitika zomwe zimasokoneza machiritso ndimamasulidwe. Ndikofunika kwambiri kumvetsa zimenezi kuti mukathe kuthandiza ena kuti athane nazo kuti akathe kulandira machiritso. Nao machitachita amenewa:

KUSOWA CHIPHUNZITSO

Kusowa chidziwitso chokhudza machiritso, ndondomeko zake, kochokera, mmene tingagwiritsire ntchito chikhulupiriro, ndi mmene tingalandirire zimasokoneza machiritso. Mulungu anati:

Anthu anga akuonongeka chifukwa chosadziwa. (Hoseya 4:6)

Yesu anati timalakwitsa ngati sitikumvetsa mau a Mulungu ndi mphamvu Yake.

Koma Yesu anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa a osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu. (Mateyu 22:29)

Anthu ena salandira machiritso chfukwa samavetsesa mau a Mulungu ndi mphamvu Yake.

Chikhulupiriro chamachiritso chimabwera pakumva Mau a Mulungu okhudzana ndi machiritso (Aroma 10:17). Baibulo limawatchula Mau a Mulungu kuti mbeu. Anthu ena amayesera kukolola kholola la machiritso popanda mau amachiritso kubzalidwa mmitima mwao. Mbeu singagwire ntchito ngati sili mwaife. Asananene kuti “Ndine Mulungu amene ndimachiza,” Mulungu koyamba anati, “Ngati azakhazikika Mmau anga.” Mau amabweretsa machiritso.

Ndi anthu angati omwe angapululumuke ngati sanamve Uthenga Wabwino wa chipulumutso? Kapena ndi angati omwe angapululumuke ngati mfundo zikulu zikulu za chipulumutso uthenga wake unali:

- Mwina sichifuniro cha Mulungu kukupulumutsani.
- Machimo anu ndi amabweretsa ulemero kwa Mulungu.
- Tsiku lachipulutso linali lakale.

Ngakhalenso timamva mayakhulidwe okhudzana ndimachiritso omwe ndimbali imodzi yomwe Yesu anaziperekerera:

- Mwina sichifuniro cha Mulungu kukuchizani.
- Matenda anu ndi ulemero wa Mulungu.
- Masiku amachiritso anapita kale.

Anthu akuyenera kuphunzidiwa Mau a Mulungu okhudzana ndi machiritso monga ngati momwe amaphunzitsidwira chipulumutso. Ndi mbeu ya Mau a Mulungu yomwe imabweretsa machiritso.

KUSAKHULUPILIKA

Chochitika china chomwe chimasokoneza machiritso ndi kusakhulupirira. Kusakhulupirira kukhoza kuchokera ku...

- Kuganiza kuti Mulungu sangachize.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, koma akhoza kusakha wosandichiza ine.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, ndipo akuyenera kundichiza, koma osati pano.
- Zotizungulira zomwe zimabweretsa kusakhulupirira zomwe zimaletsa machiritso.

Pali zitsanzo zambiri m’Baibulo za zomwe kusakhulupirira kumatchingira ntchito ya Mulungu. Mu mzinda wa Nazaleti Yesu...

Ndipo Iye, cifukwa ca kusakhulupirira kwao, sanacita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)

Yesu anazizwa, kapena kudabwa, kuti anthu sanakhulupirire:

Ndipo anazizwa cifukwa ca kusakhulupirira kwao... (Marko 6:5-6)

Baibulo limati:

Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo.

Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njira zace zonse. (Yakobo 1:6-8)

Baibulo limati, “Zizindikiro izi zizawatsata onse okhulupirira.” Vesi imeneyi ikuyakhula za okhulupirira (Kachisi). Vesi imeneyi sikunena kuti “iye amene akukhulupirira,” kunena za munthu. Sichinali chikhulupiriro cha mmodzi kapena awiri olalikira chomwe chinabweretsa machiritso omwe analembedwa mu buku la Machitidwe. Chinali chikhulupiriro cha mpingo odzadzidwa ndi Mzimu.

Ngati Yesu sanachite zozizwa ku Nazaleni chifukwa chakusowa chikhulupiriro kwawo, kodi sichimodzimidziso kunena kuti kusowa chikhulupiriro kwanthu kumatchinganso machiritso? Lero mpingo ukutsutsana kwambiri ndizomwe mpingo woyamba unachita popambana podalira pemphero. Sanavomerezebe maganizo a Baibulo pokhudzana matenda. Sanaphunzitsidwepo Mau a Mulungu zokhudzana machiritso. Koma amalozza dzala onse amene akulephera kulandira machiritso ndipo amalozza dzala onse amene akuyesetsa kutumikira machiritso. Onse omwe amalalikira Uthenga Wabwino wamphumphu wachipulumutso ndi machiritso ndi mamasulidwe zinalephereka kuti zichitike ku “Nazaleti wosakhulupirira.

KUSOWA CHIKHULUPIRIRO

Kusakhulupirira ndi khalidwe lakuti Mulungu sangachite kapena sadzachita kena kalikonse. Kusakhala wosakhulupirira sikutathauza kuti uli ndichikhulupiriro. Mwachitsanzo, amene amati kulibe Mulungu. Okhulupirira ali ndi chikhulupiriro. Kusowa kusakhulupirira kwa anthu anzeru sikutathauza kuti ndekuti ali ndichikhulupiriro.

Pakuyenera kuti chikhulupiriro chamwa Mulungu chilowe mmalo mwa kusakhulupirira chifukwa ndi pemphero lachikhulupiriro lomwe limamudzutsa munthu wodwala (Yakobo 5:15). Mukuyenera kukhala ndi chikhulupiriro, kuyakhula mau achikhulupiriro, ndi kuchita mwachikhulupiriro. Mukuyenera kuyenda ndi chikhulupiriro osati zowoneka (kuyang’ana mmene thupi liriri kapenaso zizindikiro zake).

Satana amayesetsa kuletsa machiritso pokupangitsani kuti muziyenda ndizowonka ndi maso mwala ndi chikhulupiriro. Amakupangitsani kuti muzikhala ndichidwi pa zizindikiro.

Amakupangitsani kuti muziyang'ana kwa ena omwe amanena kuti achiritsidwa, koma sanachiritsidwe. Sichikhulupiriro chomwe chiri mwa inu kapena chikhulupiriro mu chikhulupiriro cha ena. Chikhulupiriro pachokha sichimachiritsa. Ndi Mulungu amene amachiritsa. Paulo anazindikira kuti olumala anali ndi chikhulupiriro chicmene chinampanga kuti achiritsidwe ndi Mulungu (Machitidwe 14:8-10)

Sizimatengera kukhala ndichikhulupiriro chachikulu kuti muchiritsidwe. Yesu anati chikhulupiriro changati mbeu ya mpiru chinali champhamvu kwambiri. Yesu amkakumana ndi anthu malingana ndi chikhulupiriro chawo. Pamene amkamva kuti akuyenera kupezeza ndi thupi lake, Amkapitako. Pamene anali ndi chikhulupiriro sikunali kofunika, Amkangoyakhula mau kuchokera patali ndipo machiritso amkachitika.

Pamene odwala sanmachiritsidwe, anthu nthawi zambiri amalozza dzala kusowa chikhulupiriro kukhala chifukwa. Koma pamene mukuphunzira phunziro lino, pali machitachita ena amene akuyenra kuti awaunikiridwe. Yesu sanaweruze anthu amene amkafuna machiritso chifukwa chopanda chikhulupiriro.

TCHIMO LA ENI LOSALAPIDWA

Baibulo limatsimikiza ubale wachindunji omwe ulipo pakati pa tchimo la munthu ndi matenda nthawi zina:

Cifukwa cace mubvomerezane wina ndi mnzace macimo anu, ndipo mupempherere wina kwa mnzace kuti muciritsidwe. Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidweace. (Yakobo 5:16)

Davide anati, "Ngati ndibisa zolakwa mu mtima mwanga, Ambuye sazandimva ine."

Mulungu sanalonjeze kuwononga nthito za mdyerekezi mthupi mwathu pamene tikukakamirabe ku ntchito za mdyereki mmoyo mwathu. Ngati muli chodetsa mu mtima mwa munthu yemwe akudwala, akhoza wosachiritsidwa. Ngati muli machimo mu mtima mwa yemwe akutumikira, machiritso akhoza osachitika chifukwa Mulungu amakhala asakiumumva.

Mzimu osakhululuka kapena kusunga mangawa kumatchinga machiritso. Yesu anati, "Ngati simukhululukira anthu zolakwa zawo, ndekuti Atate wanu wakumwamba sangakukhululukireni zolakwa zanu." Ngati Mulungu sangatikhululukire zolakwa zanthu pamene ife sitikukhululukira ena, sangatichiritse, chifukwa machiritso amakhudzaso kuyeretsedwaso kwa moyo, mzimu ndi thupi.

KUKANA KUYERETSEDWA

Yesu anafunsa munthu wolumala pathamanda la Betisayida:

Ufuna kuciritsidwa kodi? (Yohane 5:6)

Nthawi zambiri timangofuna machiritso kapena mamaslidwe okha. Mulungu akufuna kuthana ndi munthu yense ndikumuchiza thupi, moyo ndi mzimu. Chifukwa munthu ndi thupi, moyo, ndi mzimu, mfundo yawanthunthu ikuthauza kukhudza zonsezi. Sitingakhazikike pa machiritso akuthupi mkusiyapo moyo ndi mzimu, machiritso kupatulachipulumutso.

Mulungu ndi mzimu. Amalumikizana nanu kupyolera mu mzimu wanu. Mzimu wanu umatsogolera umoyo wanu wakuntupi. Moyo wanu onse umatsamira kwambiri pa uzimu wanu. Chifukwa inu ndi munthu amene muli wauzimu. Machiritso athupi amayambira ku umzimu.

Pomwe Mulungu analenga munthu, mzimu wake unayenera kumatsogolera mphanvu za moyo wake pano pa dziko la pansi. Umayenera kukhala ndi ulamuliro pa maganizo ndi thupi lake ndikulunganizitsa munthu yense momwe Mulungu akanakhalira. Pachiyambipo, mmunda wa Eden, munthu ali paubale wabwino ndi Mulungu.

Machiritso ndiopasa kungokhala opanda matenda. Ndi nthanzi la thupi. Ndikubwereranso kukugwira ntchito kwa chiwalo chirichonse cha thupi (thupi, moyo, mzimu, kuphatikizapo maganizo, maganizo ndizina zotero)

KUSOWA KWA CHIGANIZO NDI ZOFUNA

Yesu anafunsa munthu wopuwala pa thamanda la Betesda:

“Ufuna kuchiritsidwa kodi?” (Yohane 5:6)

Pamenepa munthu wolumalayo anayenera kupanga chiganizo. Anthu samafuna kuchiritsidwa. Amakodwera akamamveredwa chisoni ndi chidwi chimene amalandira chifukwa chakudwala kwawo. Ena amalandila chithandizo cha makhwala kupyolera pakupuma pantchito kapena kudzera malamulo ndipo samafuna kuti ataye zimezo. Ena amakhala ndi kufunitsitsa kuti apite kukakhala ndi Ambuye ndiye safuna kuchiritsidwa

MABVUTO OKHUDZANA NDI KUPEMPHA KWANTHU

Pali mabvuto ambiri okhudzana ndikupempha kwanthu kwa machiritso zomwe zikhoza kutchinga kuwonetseredwa kwake:

KUSAPEMPHA:

Choyambirira cheni cheni, ndiponso chofunikira, nchakuti nthawi zina sitimapempha machiritso. Timapita ku makhwala kukafuna nthandizo kapena kwa abale kuti atitonthoze.

Mulibe kanthu chifukwa simupempha... (Yakobo 4:2)

KUSAPEMPHA MWACHINDUNJI:

Nthawi zina, mapemphero amatchingidwa chifukwa samakhala achindunji:

Mupempha koipa... (Yakobo 4:3)

Ngati mukupepha molakwika, mapephero anu ndekuti sanali achindunji. Simugwetse chandamale.

KUPEMPHA NDI CHOLINGA CHOLAKWIKWA:

Nthawi zina timapemphera ndicholinga cholakwika:

Mupempha ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukachimwaze pochita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Anathu ena amafuna kuchiritsidwa, koma osafuna kuleka njira zawo zamachimo, zakudziko, ndi moyo ochita zoipa. Amafuna akhale bwino ndicholinga choti akapitirize kuchita zinthu zawonzo. Anthu akuyenera kulingalira funso iri: “Kodi cholinga nchani chofunira kuchiritsidwa? Kodi ndicholinga chofuna kubwerera kumoyo oipa omwe mmakhala? Kapena ndicholinga choti muzithamangathamanga kuchita ntchito zabwino malo okwaniritsa cholinga chomwe Mulungu alinacho painu?”

MAPEPHERO ANU AMATCHINGIDWA:

Bible limawonetsera zinthu zina zambiri zomwe zingathe kutchinga kuti musalandire yankho la pemphero:

- Tchimo la nthundu wina uliwonse: Masalimo 66:18; Miyambo 28:9; Yesaya 1:15;59:1-2
- Mafano mu mtima: Ezekieli 14:1-3
- Mzimu wosakhululuka: Marko 11:25; Mateyu 5:23
- Kuzikonda, zolinga zolakwika: Miyambo 21:13; Yakobo 4:3
- Kumuchitira nkhaza munthu amene ulinaye pabanja: 1 Petro 3:7
- Kuzyeretsa nokha: Luka 18:10-14
- Kusakhulupirira: Yakobo 1:6-7
- Kusakhala mwa Kristu ndi Mmau Ake: Yohane 15:7
- Kusowa chifundo: Miyambo 21:13
- Chinyengo, kunyada, kubwerezabwereza kopanda pake: Mateyu 6:5; Yobu 35:12-13
- Kusapempha molingana ndi chifunilo cha Mulungu: Yakobo 4:3
- Kusapempha mu dzina la Yesu: Yohane 16:24
- Chotchinga chochokera kwa satana: Daniele 10:10-13; Aefeso 6:12
- Kuthanga kaye Ufumu: Mateyu 6:33

KUSAPIRIRA

Nthawi zina sitipirira (Kupitirizabe) kupemphera kopitirizabe. Paulo yekha pachiyambi amkalalikira akudwala (Agalatiya 4:13-14) ndipo anachiritsidwa patsogolo pake. Pemphero silinagwire ntchito mwachanguchangu pa Epafrodito (Afilippi 2: 27) ndi Trofino amene anasiyidwa (2 Temoteo 4:20). Komabe pamapeto ake onsewa anachiritsidwa. (Dziwaniso kuti

Paulo anapitiriza kupemphera chifukwa chakudwala kupatula kuti pa matenda awa panalibe machiritso ansanga).

Anth ena amaganiza kuti ngati ungapemphe machiritso kambirimbi ndikusowa chikhulupiro. Yesu sanaphunzitse kuti kukakamira pakupemphera kumawonetsa kusowa chikhulupiro. Analimbikitsa zimenezi. Luka 11:1-13 amaphunzits akufunika kwa kukakamirabe m' mphephero mu fanizo la m'bale okakamira (vesi 5-8) za mkazi wamasiye ndi oweruza (Vesi 1-8). Danieli ndi chitsanzoso chomwe chimalimbikitsa kupirira. Mulungu anamva pemphero lake poyamba pomwe, koma satana anatchinga mngero yemwe amkabweretsa yankho.

Musaleke ngati machiritso sanabwere panthawi yoyamba imene munapemphera. Kumbukirani kuti pali “kupempha, kufuna, ndikugogoda” milingo ya mapemphero. Nthawi zina umapempha ndipo yankho lapompopompo limabwera. Nthawi zina mukuyenera kufunafuna ndikupitiriza kugogoda musalandire yankho kumapemphero ena. Mneneri Elisha anapemphera kuti moti otsike kumwamba. Nthawi ina anapemphera kasanu ndi kawiri kuti mvula ibwere.

Pitirizani kupirirabe mupemphero kufikira mutazindikira kuti pempho lanu lamveka. Pamene mwakhala ndi chitsimikizo chimenechi mu uzimu mwanu, kaneko yambani kumutamanda Mulungu ngakhale kuti yakho lowonoka ndimaso silinafike.

- Jehosafati ndi ana a Israeli anayamba kumulemekeza Mulungu mofuula asanayambe kuona yankho la mapemphero awo.
- Yesu anayamba kuthokozeratu Mulungu chifukwa chomuukitsa Lazalo.
- Pamene Abrahamu anali ndichitsimikizo cha mwana, sanapitirize kumangopemphera. Anamkulupirira ndikuyamba kumukweza Mulungu.

KUSAMVERA NDONDOMEKO YAMACHIRITSO

Nthawi zina Mulungu amapereka malangizo apaderadera mundondomeko yamachiritso. Mwachitsanzo, kupyolera mwa mneneri Elisa, Mulungu anamuza Namani kuti apite kukasamba mu mtsinje wamatope kuti alandire machiritso (2 Mafumu 5:1-14). Nthawi zina kumvera kophweka ndikomwe kuli pakati pa inu ndi chozizwa chanu.

KUZINDIKIRA THUPI LA KRISTU MULAKWIKWA

Werengani 1 Akorinto 11:27-30. Kutu mukhale ndichithuzithuzi chabwino muwerengenso Luka 22:2-20, Mateyu 26:27-29, ndi Marko 14:22-25. Kufoka ndi kudwala ndizotsatira chifukwa sitilandila thupi la Kristu moyenera. “Kuzindikira: ndiko kuphunzira ndi kumvetetsa chithu pochiyesa, kufufuza, ndi kuchizindikira bwino.

Tikhoza kulephera kuzindikira Thupi la Kristu mu njira zitatu:

TANTHAUZO LA MWANZI NDI THUPI:

Timalephera kuzindikira pamene sitikumvetsa tanthauzo la chipatso champesa ndi mkate zomwe ndi zifanifani za mwanzi ndi thupi Lake. Izi ndizomwe zinachitika pamene Yesu anaphunzitsa chiphunzitso chimenechi pa Yohane 6:66 ndipo ambiri anabwerera kumutsatira Iye. Sanamvetsetse tanthauzo la uzimu pazomwe amkaphunzitsa. Pamene ambiri akuzindikira mwanzi ochotsa machimo, kawirikawiri samazindikira tanthauzo lake leni leni la jthupi. Thupi linali lobweretsa machiritso, ndetikhoza kulidya ndipo titha kuchiritsidwa. (Onani Yohane 6:48-58 ndi Luka 6:48-51).

KUGAWANIKANA M'THUPI:

Nthawi zina timalephera kuwazinfikira abale ndi alongo amene ali mbali imidzi ya thupi la Kristu ndipo kugawanikana kumakhachitika m'mkachisi. Timadya ndikumwa mosayenera ngati sititimazindikira ubale wanthu ndi abale ndi alongo mwa Ambuye. Paulo anafotokoza pa 1 Akorinto 3:1-13 kuti akhrisitu ozikonda sangadye nyama (thupi) la Atate chifukwa chakuzikonda kwawo.

KUDYA MOSAYENERA:

Timadya mosayenera pamene tikudya mgonero ndi moyo osaziyesa. Kufoka ndi kudwala ndizotsatira zake. Ichi nchifukwa chake Paulo ananena kuti kuziyensa nokha mwauzimu ndikulapa tisanadye mgonero.

MZIMU WOYIPA SUNATULITSIDWE

Ena samalandira machiritso chifukwa mtenda yawo ndi ntchito ya mzimu woyipa umene ukuyenera kutulitsidwa. Amafuna pemphero lolimba kuposa lamachiritso. Mu nyengo zimene zinabweretsedwa ndi mzimu woyipa, Baibulo linalimba kuti mdani anatulutsidwa kuti machiritso achitike.

KUSOKONEZA MALAMULO ACHILENGEDWE

Mulungu yemweyo anati “Ine ndine Mulungu amene nakulichiritsa” anaperekanso malamulo aumoyo ndi ukhondo kwa anthu Ake. Anthu ena samalandira machiritso chifukwa amasokoneza amalammulo achilengedwewa. Mwachitsanzo, munthu kumapitiriza kumwa mowa nde mkumadabwa kutnchifukwa chani machiritso okhudza ndi thenda yachiwindi sakuchitika. Akhoza kumapitiriza kusata fodya mkumadabwa kuti nchifukwa chani matenda a khansa ya mapapo sakuchitika.

NTHAWI YOYIKIKA YAKUFA

Baibulo limaphunzitsa kuti pali nthawi yoyikika yakufa (Mlaliki 3:4 ndi Ahebri 9:27). Ngakhale mneneri wamphamvu Elisa, amene anachita zozizwa zamachiritso ndikumasula,” anadwala matnda amene anamutengera ku imfa” (2 Mafumu 13:14). Muphunzira mmene mungathanirane

ndi zotchinga zimenezi pamene muzaphunzire mmene mungatumikirire kumatenda akulu monga ngati mbali imodzi yamalangizo a momwe mungatumikirire machiritso mu chaputala 8.

KUKUMBUTSA KOMALIZA

Tinatsekula phunziro lino ndimafunso ambiri:

Ndimachitachita ati omwe amasokoneza machiritso? Nchifukwa chani anth ambiri sachiritsidwa? Nchifukwa chani ena amachiritsidwa pamena ene ayi? Nchifukwa chani achikunja ndi ena owoneka ngati akhrisitu amachiritsidwa pomwe anthu achilungamo ndiozipereka sanalandirebe machiritso?

Machitachita omwe mwaphunzira mu phunziro lino ndizochitika zina zomwe zingathe kusokoneza machiritso ndimamasulidwe. Nthawi zonse kumbukirani kuti...

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)

Chikhulupiriro chimafunikira: Chikhulupiriro. Ngati muli ndimayankho onse, simungamufune Mulungu ndi chikhulupiriro. Mulungu yekha amafunsa kuti muchite mwachikhulupiriro pa Mau Ake, osati kupereka mayankho.

Pomaliza, nayo mfundo yokhudzana ndi machitachita amachiritso. Inapangidwa ndi mtumiki wotchuka yemwe anatumikira kwa zaka zambiri pa machiritso ndi mamasuridwe:

“Ine ndekha, zalalikira Uthenge Wabwino onse ngati zawone munthu wosapulumsidwa kapena kuchiritsidwa ngati ndiri ndi moyo. Ndakozeka kukhazikitsa chiphunzitsa changu pa Mau a Mulungu osasitha, osati zochitikachitika.” -F.F. Bosworth

KUSAKHULUPILIKA

Chochitika china chomwe chimasokoneza machiritso ndi kusakhulupirira. Kusakhulupirira kukhoza kuchokera ku...

- Kuganiza kuti Mulungu sangachize.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, koma akhoza kusakha wosandichiza ine.
- Kuganiza kuti Mulungu angachize, ndipo akuyenera kundichiza, koma osati pano.
- Zotizungulira zomwe zimabweretsa kusakhulupirira zomwe zimaletsa machiritso.

Pali zitsanzo zambiri m’Baibulo za zomwe kusakhulupirira kumatchingira ntchito ya Mulungu. Mu mzinda wa Nazaleti Yesu...

Ndipo Iye, cifukwa ca kusakhulupirira kwao, sanacita kumeneko zamphamvu zambiri. (Mateyu 13:58)

Yesu anazizwa, kapena kudabwa, kuti anthu sanakhulupirire:

Ndipo anazizwa cifukwa ca kusakhulupirira kwao... (Marko 6:5-6)

Baibulo limati:

Koma apemphe ndi cikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo.

Pakuti asayese munthu uyu kuti adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njira zace zonse. (Yakobo 1:6-8)

Baibulo limati, “Zizindikiro izi zizawatsata onse okhulupirira.” Vesi imeneyi ikuyakhula za okhulupirira (Kachisi). Vesi imeneyi sikunena kuti “iye amene akukhulupirira,” kunena za munthu. Sichinali chikhulupiriro cha mmodzi kapena awiri olalikira chomwe chinabweretsa machiritso omwe analembedwa mu buku la Machitidwe. Chinali chikhulupiriro cha mpingo odzadzidwa ndi Mzimu.

Ngati Yesu sanachite zozizwa ku Nazaleni chifukwa chakusowa chikhulupiriro kwawo, kodi sichimodzimodzisokunena kuti kusowa chikhulupiriro kwanthu kumatchinganso machiritso? Lero mpingo ukutsutsana kwambiri ndizomwe mpingo woyamba unachita popambana podalira pemphero. Sanavomerezebe maganizo a Baibulo pokhudzana matenda. Sanaphunzitsidwepo Mau a Mulungu zokhudzana machiritso. Koma amalozza dzala onse amene akulephera kulandira machiritso ndipo amalozza dzala onse amene akuyesetsa kutumikira machiritso. Onse omwe amalalikira Uthenga Wabwino wamphumphu wachipulumutso ndi machiritso ndi mamasulidwe zinalephreka kuti zichitike ku “Nazaleti wosakhulupirira.”

MAYENSO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la machiritso osawonera.

2. Perekani tanthauzo la mau oti “machitachita.”

3. Papepala lapadera lembani mwachidule zokhudzana machitachita otsatirawa amene amatchinga machiritso:

Kusowa kwachiphunzitso
Kusakhulupirira
Kusowa chikhulupiriro
Kusowa mphamvu
Tchimo la inu eni losalapidwa
Kukana kuti mukozedwense
Kusowa kopanga chiganizo ndi chikhumbokhumbo
Mavuto okhudzana ndi kupempha
Kusowa chipiriro
Kusamvera mundondomeko yamachiritso
Kusazindikira thupi la Kristu
Kusatulitsidwa kwa mizimu yoyipa
Kukopera ntchito ya Mulungu
Kumphanya malamulo achilengedwe cha Mulungu
Nthawi yoyikika yakufa

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwabukuli)

KUCHITA MAWU

1. Phunzirani zambiri zokhudzana cholinga cha Baibulo pazumphumphu.
 - Pamene anthu amkangofuna machiritso okha, Yesu amakafuna kuthana ndi munthu yense wanthunthu. Anati kwa munthu olumalama pa nthamando la Betisida, “Kodi ukufuna kuchiritsidwa?”: Yohane 5:6.
 - Yesu anabwera kuzatumikira kwa onse amene anali odwala, osweka, odwala, oponderezedwa: Mateyu 9:12; Marko 2:17; Luka 5:31.
 - Yeu anali gwero la ugwiro: Yohane 5:15; Machitidwe 9:34
 - Ambiri amene anamukhudza Iye anachiritsidwa: Mateyu 9:21-22; 14:36; Marko 5:28-34
 - Yesu anamchiritsa kapolo amene anali pakama la imfa: Luka 7:10
 - Anachiritsa wopuwala: Yohane 5:9
 - Kupyolera mu mphamvu ya Mulungu, okhulupirira anachiritsa wolumala: Machitidwe 9:34
 - Yesu anachiritsa wodwala: Mateyu 5:31
 - Anabwezeretsa manja: Mateyu 12:13; Marko 3:5; Luka 6:10
 - Anawachiza anthu kunthenda zawo zosiyanasiyana zomwe anali nazo: Yohane 5:6
 - Anachiritsidwa kotheratu: Yohane 7:23
 - Yesu anakondwera ndi chikhulupiriro cha anthu kuti ndichamoyo kumbali yochiritsidwa. “Chikhulupiriro chanu chakuchiritsani.” : Mateyu 9:22; Marko 5:34; 10:52; Luka 8:48-50; 17:19
2. Werengani mau a chigiriki Muchipangano Chatsonapo amene amatanthauza kuti “kukozedwa”

Mfotokozi:

Holos: Onse, pamodzi, payekhayekha.

Pas: Onse

Hapas: Onse, kukozedwa

Holokleros: Yense, Konse.

Hugies: Kupanga odwala kutiatsatire kuyimba kwanthu: Mateyu 12:13; 15:31; Marko 3:5; 5:34; Luka 6:10; Yohane 5:4,6,9,11,14,15; 7:23; Machitidwe 4:10
Holoteles: Ugwiro, umphumphu, kumaliza: 1 Atesalonika 5:23. Kufikira mbali zonse za munthu.

Mneni:

Hugiaino: kukhala mu umoyo wabwino; amene achiritsidwa; amphumphu, anthazi, ochiritsika.

Sozo: kupulumutsa, kuchiritsa.

Iaomai: Kuchiritsa; kutumidwa kukachiza.

Ischuo: Kukhala wa mphamvu.

Diasozo: Kpulumutsa motheratu.

3. Lingalirani funzo iri: Kodi nchni chikukusungani inu ku umphumphu mthupi, malingaliro ndi mzimu?
-

4. Kodi makhulupirira china chake mwazotchinga zotsatirazi zimene zimasokoneza machiritso anu kapena a munthu wina wake amene mukumutumikira? Onani zimene zikugwirizana

- Kusowa kwachiphunzitso
- Kusakhulupirira
- Kusowa chikhulupiriro
- Kusowa mphamvu
- Tchimo la inu eni losalapidwa
- Kukana kuti mukozedwenso
- Kusowa kopanga chiganizo ndi chikhumbokhumbo
- Mavuto okhudzana ndi kupempha
- Kusowa chipiriro
- Kusamvera mundondomeko yamachiritso
- Kusazindikira thupi la Kristu
- Kusatulitsidwa kwa mizimu yoyipa
- Kukopera ntchito ya Mulungu
- Kumphanya malamulo achilengedwe cha Mulungu
- Nthawi yoyikika yaku

5. Potengera zimene mwaphunzira mu phunziro lino, bwererani ku ndandanda wachinayi mwambamo ndipo mulembe mmen mungayakhire ku chotchinga china chirichonse zomwe munawona.

6. Kodi munayamba mwakhalapo ndi funso lopanda yankho pokhudzana machiritso ndi mamasuridwe? Ngati ndi choncho, chinali chani?

Kodi kenako munakwanitsa kumvetsetsa_____ngati ndi choncho, fotokozani mmene funso lanu linayakhidwira:

Ngati ayi, ndipo inu munakalibe ndi mafunso okhudzana ndi nyengo yakuthupi, kumbukirani lonjezano la phunziro lino.

Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (1992 Deuteronomo 29:29)

7. Kodi zotsatirazi zimatchinga pemphero lanu lamachiritso? Onani zonse zimene zikugwirizana:

- Tchimo la ntundu wina uliwonse
- Mafano mumtima mwanu
- Mzimu osakhulupirira
- Kuzikonda, zolinga zolakwika
- Njala yamphamvu
- Kuzuza nzanu amene muli naye pa banja
- Kuzilungamitsa nokha
- Kusakhulupirira
- Kusakhala mwa Khristu ndi Mau Ake
- Kusowa chifundo
- Chinyengo, dama, kumangobwereza zopanda pake
- Kusapempha molingana ndi chifuniro cha Mulungo
- Kusapempha mu dzina la Yesu
- Zotchinga zasatana
- Kusayamba mwafuna kaye Ufumu

Kodi mungatani kuti mukonze mavuto amenewa?

GAWO LACHISANU

NDONDOMEKO ZAMACHIRITSO

Mugawu lino muphunzira ndondomeko zotumikirira ndi kulandira machiritso. Muphunzira zokhudzana:

- **MMENE MUNGATUMIKIRE NDI KULANDIRA MACHIRITSO.**
- **UTUMIKI OLONDOLA ONSE AMENE ACHIRITSIDWA**
- **MACHIRITSO AMTHERADI**

Kumbukira machitidwe a Ufumu wa Mulungu amene mwaphunzira kumayambiro kwa phunziro lino: Pamene mwayamba kutumikira machiritso, machiritso amakutumikirani inu.

CHAPUTALA 14

UTUMIKIRA MACHIRITSO

ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kufotokoza zokozekera zoyamba pautumiki wa machiritso.
- Kulemba mwachidule ndondomeko zotumikirira machiritso.

LONJEZANO LA MACHIRITSO:

Ndipo pamene mulikumuka lalikirani Ufumu wa kumwamba wayandikira

Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwa ulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)

CHIYAMBI

Mwaphunzira kuti machiritso ndi mamamasuridwe ndi machitachita a Ufumu wa Mulungu. Mu phunziri lino muphunzira mmene mungatumikirire machiritso. Muphunziro lotsatira muzaphunzira mmene mungatumikirire mamamasuridwe.

ZOKOZEKERA ZOYAMBA

Chikhulupiriro chimadza pakumva Mau a Mulungu okhudzana machiritso. Kuti mukulitse chikhulupirio chanu, mukuyenera kuphunzira china chirichonse chamachiritso chomwe chiri m’Baibulo. Werengani Chipangano Chatsopano ndi maganizidwe atsopano. China chirichonse chimene Yesu anawauza omutsatila kuti achite, inuso mukuyenera kuchita zimenzo. Zonse zimene anati achita, yembekezeni kuti achita.

ZIKOZEKERETSENI NOKHA:

Ngati anati mukhoza kuchiza odwala kupyolera mu mphamvu yake, ndeyembekezerani kuona iwo akuchizidwa. Ngati anati muzatulutsa ziwanda, nde chitani izi kupyolera mu dzina Lake ndipokhulupirirani kuti zikumverani. Kanani ziphunzitsa zonse za munthu zomwe munalandira. Khulupirirani kuti Chipangano Chatsopano chimachita zonse zomwe chimanena. Chimvomerani kuti ndichoona ndipo chitani moyenerera. Ndinu kazembe wa Keistu (2 Akorinto 5:20). Kazembe samakaika kuti dziko lomwe akuliimirira liikira kumbuyo mau ake.

Salani kudya ndi kupemphera musanayambe kutumikira. Onani chitsanzo cha Paulo pa Machitidwe 28:8. Popeza mphamvu ndi ulamuliro ochiritsa umachokera kwa Mulungu, ndendikofunika kuti pakhale kulumikizana kwambwino. Kuzuzidwa kwina ndi ziwanda kuzachiritsidwa paakupemphera ndikusala kudya. Yesaya 58 imaphunzitsa kuti Mulungu amalemekeza kusala kudya komwe kumaika chidwi pazofuna za ena.

Yambani kutumikira kwa odwala ngakhake kuti simukumvetsetsa chinachirichonse zokhudzana ndi machiritso akumwamba, monga ngati momwe munayambira kuchitira umboni pomwe munapulumutsidwa ngakhale kuti mumkhayenera kuphunizra kaye zokhudzana ndi moyo wa Chikristu. Yambani kutumikira kuyambira pazomwe madziwa zokhudzan ndi machiritso. Pomwe mukuyenda mukuwala komwe mwapatsidwa, muzalandira kuwala kwambiri. Tengani maganizo oti kulibe nyengo yopanda chiyembekezo. Pali anthu omwe akhala opamba chiyembekeze za izo.

ZOKOZEKERA ZOYAMBA KWA ENA:

Ngati malimbikitsa odwala kuti apephereredwe popanda malangizo oyerenerera, zilingati kumulimbikitsa munthu wosapulumuka kuti alandire Yesu kukhala mphulumutsi wake popanda kudziwa kuti Ndindani, akuyenera kuzindikira machimo awo, ndikufunikwa kwachipulumutso chawo.

Nthawi zina, Mulungu amachiritisa popanda malangizo oterewo. Koma kumbukirani: Potumikira machiritso, mukuyenera kugwiritsa bwino ntchito njira zonse zimene mau a Mulungu anapereka kuti muwone mmene ntchito itachitikire. Chikhulupiriro ndi njira imodzi imene mphamvu ya machiritso a Mulungu imabwerera ndipo imabwera ndi mau amachiritso. Nde malangizo ndi ofunika. Yesu anasakaniza kulalikira ndi kuphunzitsa ndi machiritso ndipo analamula Omutsatira Ake kuchachitaso chimodzimodzi.

Anthu akuyenera kudziwa chimene mau a Mulungu amanena kwa komwe kumachokera machiritso, gwero ndi choyambitsa chatatenda, malonjezano amachiritso, ndi ndondomeko za Baibulo zolandirira machiritso ndimmene tingakhalire anthanzi.

Pandondomeko yopereka machiritso kwa okhulupirira, kusala kudya ndi kupephera kwa odwla kukhoza kukhala kothandiza. Izi sizofunika kuti machiritso abwere, koma kumbukirani-tikuyenera kugwiritsa ntchito njira ina iriyonse yopezeka m’Baibulo. Mulungu anatsimikiza zakupempha kwanthu ndipo Yesaya 58:6-8 imatsimikiza za kufunika kwa kusala kudya ndi kupemphera pokhudzana ndi umoyo wabwino.

NTHAWI YAUTUMIKI

Nawo malingaliro azomwe ziyenera kuchitika pa nthawi yotumikira machiritso. Kumbukirani izi ndi ndondomeko chabe. Mukuyenera kumvomera chitsogonzo chosiyanasiyana chochokera kwa Mzimu Woyera. Ena mwamalingalirowa amangogwira ntchito kwa anthu ochopa akutumikiridwa, pamene ena amagwira ntchito potumikira ku gulu la anthu:

KUPANGA MALO ACHIKHULUPIRIRO:

Pangani malo achikhulupiriro. Munayamba kale kuchita zimenezi pomwe matumikira Mau pa machiritso, koma mukufunikaso kutenga mkwerero lina popanga malo achikhulupiriro. Azungulireni odwala ndi anthu achikhulupiriro ndi otsimikizika mtima. Lolani kuti amve maumboni a anthu onse amene anachiritsidwapo. Kumbukirani kuti kusowa chikhulupiriro kumatchinga ngakhale utumiki wa Yesu ku Nazarete.

Machiritso akhoza kubwera kupyolera pakulambira ndi kutamanda ngakhale popanda pemphero lamachiritso chifukwa Mulungu amakhala matamando a anthu ake. Pamene tikulambira Mulungu, amapezeka kuti achiritse. Kuwasendeza anthu pa mulingo pachiganizo chamachiritso awo, monga mmene mungachirite ndichipulumutso. Kumbukirani momwe Yesu amanamfusira munthu wolumala, “Kodi ufuna kuchiritsidwa?” (Yohane 5:6).

Mufunzeni munthu kuti awonetse chikhumbokhumbo chawo chamachiritso. Pa gulu mukhonza kuwafunsa iwo kuti ayime, abwere kutsogolo, aimike manja awo, kapena kuika dzanja lawo pamalo pomwe akudwalapo pa thupi pawo. Izi zimathandiza kuti awonetse chikhumbokhumbo chawo chofuna kuchiritsidwa. Ndi kuchita kwachikhulupiriro kwa iwo, komaso izi zimakuthandizani kuzindikira onwe akufuna kutumikiridwa.

PEMPHERERANI CHIDZIWITSO:

Pemphererani nzeru ndi chidziwitso musanatumikire machiritso. Gawani nzeru ya kumwamba yomwe Wakupatsani. Mulungu anthu kukuwululirani:

Mau a chizindikiro: Mau a chidziwitso amaulula chindunji cheni cheni cha munthu kapena mmene alili nde muzazindikira momwe mungapempherere. Mau achizindikiro akhoza kumphatikizapo kuzindikira mozama, kutsikizika mu uzimu, maganizo, mau kapena maganizo. Mau a chidziwitso amatha kuvumbulutsa kuti matendawo ndi otani kapenanso kuti nchifukwa chani kuti munthu akudwala chonchi.

Vesi ya Mmau: Mulungu akhoza kukupatsani “Rhema” (apaderadera) Mau a Mulungu chifukwa cha nyengo imeneyo, matenda, munthu kapena gulupu.

Masomphenya: ichi ndi chinthunzinthunzi cha mmaso amalingaliro chokhudzana ndi omwe mukawatumikire.

Mau a chikhulupiriro: Awa ndi mau apaderadera achirimbitso ndi chikhulupiriro makamaka kwa munthu ameneyo.

Kudzodza kwapaderadera: Kudzadzidwa ndi mphamvu mwadzidzi, umayamba kumva kutentha kapena umakhala ndikulimbika mtima kwambiri. Nthawi zina kudzodza kumeneku kumabwera, umayamba kuyenda nako. Koma musadikire kudzodz kwapaderaderaku kuti mupempherere odwala. Mukuyenera kutsata malangizo a Yesu kaya mukufuna kapena ayi.

Kuchita mwachikhulupiriro mwapaderadera: Nthawi zina Mulungu azakutsogolerani kukamuza munthu kuti achite zina mwachikhulupiriro zomwe zinabweretse machiritso.

KUZINDIKIRA MVUTO:

Gwiritsani ntchito uthenga pochokera pakufusa mafuso ndi nzeru zomwe Mulunguu wakupatsani kuti muzindikire ngati mvutoliri:

Lakuuzimu: Awa ndi mamvuto omwe amakhudzana ndi tchimo ndipo amafunika kutumikiridwa ndi machiritso auzimo (chipulumutso, kulapa ndi kukhululidwa kwa tchimo).

Ngati Pali gwirizano pakati pa tchimo ndi nthenda (ndipo tawona kuti palidi gwirizano), ndekuti paligwirizano pakati pa kukhilulukiridwa ndi kuchiritsidwa, ndi ntchito ya Mzimu Woyera kubvumbulutsa popeza mwantchito Yake imodzi ndi kutsutsa ndi kukuza.

Musamachite machawi polumikiza matenda ndi tchimo. Kumbukirani kuti matenda onse mwaphunzira kuti simatenda onse omwe ali zotsatira za tchimo la mwini. Ngati pali tchimo, nde ndi udindo wa Mzimu Woyera kubvumbulutsa popeza cholinga Chake ndi kutsutsa ndi kukoza.

Zakuthupi: Awa ndi matenda akuthupi, kumvulala, kapena madwale. Pempheperani machiritso akuthupi.

Maganzo: Awa ndi mabvuto monga kudera nkhawa, khwiyo, kuwawidwa mtima, kukhumudwa, kulephera, kukhala ndi chikaiko, kaduka, kuzikonda, kusokonekera, kusakhululuka, ndi zotsatira zamabvuto akale. Anthu awa akufunika machiritso amaganizo. Machiritso amenewa amatchulidwa kuti “machiritso amkati,” koma liwu lagwiritsidwa ntchito udyo ndi anthu ena. Sikofunika kupitaso pambuyo mkukayeserera zonse zomwe zinachitikazo. Sikofunika kuti pachite kutenga masabata, miyezi kapenaso zaka kuti uchire kumabvuto amenewa. Ngati mungachite zimenezi, ndekuti mukuyesera kuchiza munthu wakale mmalo momuthandiza kuti akhale olengedwa mwatsopano mwa Kristu.

Mabvuto amaganizo kawirikawiri amakhudzana ndi mmene munthu akukhalira. Amatha kusokoneza mabanja komaso ubale wa munthu. Machiritso amabwera kupyolera pakuzindikira mvuto, kupempha chikhululukiro, ndikhuwakhululukira onse omwe anatengapo gawo pobweretsa mabvutowo.

Chotchinga chachikulu cha machiritso amaganizo kawirikawiri chaimakhala kusakhululuka, nde machiritso amaganizo ndikuphatikizapo kuchiza maubwezi. Tinayitanidwa kukhala atumiki oyanjanitsa (2 Akorinto 5:18-21). Anthu akuyenera kuyanjanitsidwanso ndi Mulungu ndi munthu, ndipo apa ndipamene maganizo, maganizo ndi machiritso amkati amabwera.

Mukhoza kufuna kumuphunzitsa munthu zokhuzana ndi kukhululuka. Kukhululuka si:

- Kulungamitsa zolakwa zawina zomwe akuchitirani. (Mwachitsanzo, kunena kuti, ” pochita zimenezi anali atapanikizika.”)
- Sikukana kuti pachiyambi munamvulazidwa.
- Kukana zomwe zinachitidwa kwa inu.
- Kudikira nthawi yochiritsidwa pakumvulazidwa. (Sichoncho).

Kukhululuka kweni kweni kumabwera ndi:

- Kumvomereza kuti zomwe zinachitika kwa inu zinali zolakwika, ndizochita za anthu ochimwa mudziko la uchimo. Sikufunika kubwereraso pambuyo

kumakakumbukiranso zomwe zinachitikazo, koma mmalo mwake mukhoza kuthana nazo pozikana. Mvomerezani zomwe zinachitikazi ndi momwe zinakhudzirani.

- Perekani kumvulazidwa kwanu kwa Mulungu ndipo Mumupemphe kuti akuchiritseni kumaganizo oipa. Simungaiwaliretu choonadi cheni cheni cha zomwe zinachitika ndi mmene zinakukhudzilani koma chomwe mukufunika ndi machiritso pa zoipa pa zomwe zinakuchitikirani.
- Kumphepha Mulungu kuti akuthandizeni kukhululukira ena omwe anatengapo mbali, nde akhululukireni iwo monga momwe Kristu amakukhululukirani inu. Zindikirani kuti Mulungu akukhululukirani pamene inu mukukhululukiranso ena: “Mutikhululukire ife zolakwa zanthu monga ifenso tikhululukira amangawa anthu.” Munthu akuyeneranso kuzikhululukira yekha (kumva kulakwa pazolakwa zimene wachita) ndipo akuyenera kupempherera machiritso pa maganizo ake. Nazo ndondomeko za momwe munthu angazikhululukire yekha:
 - Mvomerezani tchimo lomwe likukupangitsani kulakwa ndi maganizo auchimo, mvomerezani kwa Mulungu, ndipo lapani. Mpempheni kuti akukhululukireni machimo anu ndipo achiritse maganizo anu.
 - Zindikirani kuti Mulungu akakhululukira, amaiwala (amawaponya kutali machimo anthu monga mmene kuliriri kutalikana kwa kummawa ndi kumadzulo).
 - Funsani 1 Yohane 1:8-9 ndi Aroma 8:1

Zamubongo: Awa ndimabvuto amene amachokera pakuganiza molakwikwa, chiwembu cha satana maganizo, kusaganiza mokwanira, ndizita zotero. Pemphererani machiritso.

Ziwanda: Izi ndi nyengo zobwera chifukwa cha machitachita aziwanda monga kugwidwa ndi chiwanda. Muphunzira mmene mungathanirane ndi zimenezi muphunziro lotsatira potumikira mamasuridwe. Nthawi zonse kumbukirani kuti mabvuto amiyamba amakhudza munthu yense. Pamene mukutumikira, chitani ndi munthu yense monga mmene Yesu anachitira, osangoti matenda okha. Munthu ndi thupi, moyo, ndi mzimu. Uthuthu ukutathauza kuchitanazo zonsenzi.

PEMPHERANI PEMPHERO LAMACHIRITSO:

Mutantha kuwona mmene ziririr, mukuyenera kupemphera pemphero lamachiritso. Koma nthawi zina, musamadabwe ngati Mulungu atakuzani kuti musapemphere kapena muchedwe kupemphera. Mwachitsanzo, kupyolera pofunsa mafunso mukhoza kuzindikira kuti munthu sakufuna machiritso chifukwa aluza cholowa chaulumali wawo (Izi zinachitika mu mkumano wina wamachiritso).

Ambuye akhoza kukuuzani kuti muchedwelepo popempherera machiritso akuthupi kufira atazakuuzaniso kapena kuti munthuyo athane kaye ndi mvuto la tchimo. Pamene mukupemphera, muzipephera pemphero lachikulupiriro lomwe limalunjika pamvuto lenileniro. Kumbukirani kuti simukuyenera kumukakamiza Mulungu kuti achiritse pakudzera kotalika ndi kukuwa kwa kupemphera kwanu. Monga kuti chipulumutso chiripo kale, izinso ziri chimodzi modzi ndi machiritso. Monga momwe kuti chipulutso chimabwera ndi chikhulupiriro, ndeziriso choncho ndi machiritso. Mulungu akufuna kuchiritsa, chimodzimodzi monga amafuna kupulumutsa.

Chifungulo cha kuyakhidwa kwa pemphero ndi kupemphero malingana ndi chifuniro cha Mulungu “Ngati ndichifuniro cha Mulungu.” Yesu sanapemphere “Chiritsani ngati chiri chifuniro Chanu.” Pempherani pemphero lakuti kufuna kwa Mulungu kuchitidwe “kufuna kuchitike monga chomwecho Kumwamba” kapena “maringana ndi chifuniro Chanu.” Uku mkuzindikira ukulu wa Mulungu.

Ngati mkotheke, ngwiritsani ntchito okhulupirira ena kuti atumikire nanu limodzi. Pamakhala kuchulukitsa kwa mphamvu ya uzimu pamene anthu ochuluka akupemphera (Onani Mateyu 18:19). Utumiki wakuthupi sumalimbikitsa anthu omwe akupambana mu mphatso za machiritso ndi onse omwe alandira machiritso mkuyamba kupereka ulemu kwa iwo eni kapena kwa munthu wina. Wina aliyense wamu thupi la Khristu alinayo mphatso imodzi ya uzimu. Utumiki wopambana ndi pomwe...

monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a cisomo ca mitundu mitundu ca Mulungu. (1 Petro 4:10)

Pemphero lanu lamachiritso likhoza kukhala limodzi mwa awa:

- Zopempherera Marko 7:32-35
- Kulamula Luka 4:38-39; Marko 7:32-35; Yohane 5:8; Machitidwe 3:6; 9:40
- Kupembedzera Machitidwe 32
- Kudzudzula ndi kutulutsa Marko 9:25

Mapemphero anau amakhudzanaso ndi malangizo kuti mukachite zinthu zina mwapaderadera, monga momwe Mulungu akufunira (Onani Yohane 9:1-7). Musamawakakamize anthu kuti aleke kumwa makhwala. Mulekeni Mulungu kuti awatsogolere Yekha kuzimenezi. Nthawi zonse pempherani mudzina la Yesu. Kumbukiraniso kuti sikusowa chikhulupiriro kupemphera kambirimbiri. (Kumbukirani zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana pakupirira popemphera.)

KUMULEMEKEZA MULUNGU CHIFUKWA CHA MAYANKHO:

Pemphero lanu lizitsatana ndi matamando kwa Mulungu chifukwa chamachiritso. Kumbukirani kuti anthu nkhumu akhate omwe Yesu anawatumikira, onse anachiritsidwa koma mmodzi yekha ndamene anabwerera kukamutamanda chifukwa chamachiritso ake. Mulungu alemekedwe ndi chikhulupiriro osati ndi maso chabe. Mwachita zomwe mau a Mulungu amakuzani kuti muchite.

Khulupirirani kuti Mulungu wachita zimene ananena kuti achita. Muthokozeni chifukwa chazimenezi. Yesu anamuthokoza Mulungu chifukwa chachiritso pemphero lomwe anapemphera Lazaro asanatuluke mmanda.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la machiritso osawonera.

2. Fotokozani zokozekera zoyamba pa utumiki wamachiritso.

3. Lembani mwachidule ndondomeko zazotumikira machiritso.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwabukuli)

KUCHITA MAWU

1. Onani zitsanzo za Yesu kufunsa mafunso kwa odwala asanatumikire machiritso:
 - Marko 5:1-20 Yesu anafusa munthu wogwidwa ndi ziwanda.
 - Marko 8:22-26 kufunsidwa kwa munthu wosawona.
 - Marko 9:14-27 Mafunso okhudzana ndi nyamata wamizimu yoyipa.
 - Marko 10:46-52 Mafunso okhudzana Batuneyo wakhungu.

2. Yesu anawaphunzitsa omutsatira Ake mu utumiki wa machiritso (Mateyu 10:18). Umu ndi mmene anapangira gulu la ogwira ntchito kuti akatumikire machiritso ndi inu:
 - Sankhani gulu la anthu antchito. Anthuwa akhale ophuzitsika, akhale ndichilakolako cha utumiki, akhale mkuthekera kotenga chitsogozo, akhale anthu achikondi ndi chifundo, ndiposo akhale anthu auzimu ndi machitidwe abwino.
 - Gwiritsani ntchito maphunziro amane ali buku lino ndi Mau a Mulungu powalangiza ndi kumanga chikhulupiriro chawo.
 - Muzikhala ndi nthawi yosala kudya ndi kupemphera.
 - Muzidziwiratu kuti ndi ndandi amene atakachite chakuti panthawi yotumikira machiritso. Musamagwiritse ntchito

CHAPUTALA 15

UTUMUMIKI WAMACHIRITSO OLONDOLA

ZOLINGA

Pamapeto pa phunziroli mukuyenera kukwanitsa izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kufotokoza chisamaliro cholondola kwa onse amene achiritsidwa.
- Kufotokoza chisamaliro cholondola kwa onse amene sanachiritsidwe.

LONJEZANO LAMACHIRITSO:

Ndipo mwa ici ali Nkhoswe ya cipangano catsopano, kotero kuti, popeza kudacitika imfa yakuombola zolakwa za pa cipangano coyamba, oitanidwawo akalandire lonjezano la zolowa zosatha.

Pakuti pamene pali copangiratu pafunika pafike imfa ya wolemberayo. (Ahebri 9:15-16)

CHIYAMBI

Ndikofunika kwambiri kuti onse amene achiritsidwa akuyenera kulandira utumika olondoledwa. Yesu anapereka malangizo oti tizilondola onse amene alandira machiritso ndi mamasulidwe.

Anayakhula ndi munthu amene anachizidwa ku khate:

Ndipo iye anamuuzitsa, kuti asanene kwa munthu ali yense; koma ucoke, nudzionetse wekha kwa wansembe, nupereke nsembe ya pa cikonedwe cako, monga adalamulira Mose, kukhale umboni kwa iwo. (Luka 5:14)

Anamuza mzimayi wochimwa amane anachiritsidwa:

Pita kunyumba kwako, nufotokozere zazikuruzo anakucitira iwe Mulungu... (Luka 8:39)

Kwa mzimayi amene anagwidwa akuchita chigololo anati:

... Inenso sindikutsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano usacimwenso. (Yohane 8:11)

Ngati mukutumikira nokha kwa munthu, mukuyenera kukhala ndi nthawi yomulondola nokha. Ngati pa msokhano waukulu, mukuyenera kupereka ulangizi mukamaliza kutumikira, kapena

mamawa wake. Ngati mukutumikira pa mpingo, afunsemi abusa kuti azilondola onse amene achilitsidwa.

Malangizo olondola akuyenera kukhudza zinthu izi:

- Tingatani kuti tikhalebe ochiritsidwa.
- Tichite chani ngati sanachiritsidwe.

TINGATANI KUTI TIKHALABE OCHIRITSIDWA:

Mphunzitsani onse omwe angochiritsidwa kuti:

Azindikire kuti ndi chiwembu cha satana:

Monga momwe satana amayesera amane wangopulumutsidwa kumene, amayesaso munthu wina aliyense amane wachiritsidwa. Monga momwe mungalepherere chipambano cha uzimu, mothanso kulephera chimodzimodzi kuthupi. China chirichonse chomwe makhulupirira Mulungu muuzimu mwanu, muzayensedwa kumbali imeneyo. Satana azakuyensani inu pa:

- Zizindikiro: Machiritso nthawi zina amachitika pang'onopang'ono. Zizinfikiro zanu mwina sizingachoke mwachangu. Zizindikiro zanu mwina zikhoza kuipirabe. Mukhoza kumatetha thupi, koma iyi ikhoza kukhala njira imene thupi likulimbana ndi matenda monga ngati mbali imodzi ya machiritso. Muzyenda ndi chidziwitso cha uzimu, osati ndi zowoneka ndi maso. Musamke kuzungulira kumalengeza za zizindikiro zanu, kwinaku musamanane pa zimenezo. Ngati mwafunsidwa muziyakha kuti "inde, ndiridi ndi zizindikiro za _____, koma ndi mikwingwirima Yake ndachiritsidwa." Muzika chidwi chanu pa zinthu zosawoneka mwalo mwa zizindikiro. Zizindikiro zikhoza kukuchotsani pa Mau a Mulungu, pa maso Pake, malonjezano Ake, ndi mphamvu Yake. Musamayakhule mau olakwikwa omwe amakweza chiwembu cha satana pathupi panu. Amena amakulibikitsani inu kwambiri-kusowa kwazizindikiro kapena Mau a Mulungu amene amanena kuti Iye ndi mchiritsi wanu? Chidwi chanu ndi chani?
- Kukupangitsani inu kuti muziyang'ana kwa ena: Kuloza kwa ena omwe amaganiza kuti anachiritsidwa, koma pano akudwalaso. Musamayang'ane kwa omwe amanena kuti anapulumutsidwa koma tsopano akukhala mu uchimo ndipo akugwiritsidwa ntchito ngati chitsanzo pokana chowonadi chachipulumutso?
- Matha: Kuwopa kuti matenda anu atha kubwereranso.
- Anthu olakwika omwe akuzungulilani: Onse amene adzadzidwa ndi kusakhulupirira omwe amadzala ambeu yachikaiko mwa inu.

Kanizani ziwembu za satana:

Muzikhalabe pamalo achikhulupiriro popitiriza kuwerengnga Mau a Mulungu amachiritso. Mulemekezeni Mulungu chifukwa chamachiritso anu. Muzilumikizanabe ndi mchiritso wanu popemphera. Chitirani umboni machiritso anu kwa ena, kupereka matando kwa Mulungu. Njira imodzi yomugonjetsera satana ndikupyolera mau a umboni wanu. Kanizani ziwembu zasatana ndi “Rhema” Mau a Mulungu potenga veis yapaderadera yokhudzana machiritso. Musamagwedezeke mchikhulupiriro chanu, munthu yemwe amangogwedezeka sazalandira kuchokera kwa Mulungu (Yakobo 1:6-8). Limbikani (Limbanani) mwachindinji mchikhulupiriro pamachiritso anu (Aroma 10:9)

Makana ziwembu za satana pamene mukugwiritsa ntchito ulamuliro wanu wauzimu omwe mkuphatikizapo:

- Mau a Mulungu.
- Mwazi wa Yesu.
- Mau a umboni wanu.
- Ulamuliro womanga kapena kumasula.
- Pemphero ndi matendo.
- Zida zakhondo zomwe ziri pa Aefeso 6:10-18.
- Ulamuliro ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

(Ngati simunabatizidwe ndi ubatizo wa Mzimu Woyera mukuyera kuusakasaka. Mzimu Woyera amaperaka mphamvu yomwe imakuthandizani kuti musungebe machiritso anu. Monga mmene mutaphunzirire mu chaputala chotsatira, izi ndi zofunika makamaka pa mamasuridwe kumachitachita aziwanda.)

Sithani kakhalidwe kanu:

Kubwereranso kumoyo wochimwa kukhoza kutanthauza kuti kubwereraso kwa matenda (Yohane 8:11). Yendani mkumvera kwa Mulungu ndi Mau Ake. Kuchimwa kwadala kukhoza kutayitsa machiritso (Yohane 5:14). Kubwereranso ku machitachita opanda pake kukhoza kuchititsaso kuti mtenda ibwerereso. Machitachita opanda pake ndi tchimo leni leni, lomwe limadetsa kachisi wa Mulungu.

Tsatirani ndondomeko za Baibulo za kukhala moyo wa nthazi ndi machiritso:

Baibulo limaperaka ndondomeko zokhalalira moyo wathanzi. Pezani phunziro la Harvestime lotchulidwa kuti “Nkhon do ya thupi” kuti muphunzire ndondomeko zimenezi mwatsatanetsatane.

Bwererani kuchipatala kuti akatsimikize kuti mwachiradi:

Ngati mwakhala kuti munali pamakhwala, bwererani kwa dotolo wanu kuti akatsimikize kuti mwachiritsidwadi. Pansi pa Chipangano Chakale, amsembe anali ngati madotolo. Amayeza matenda ndipo amkalengeza machiritso. Yesu anamuza wakhate yemwe anamuchiritsa:

...koma ucoke, nudzionetse wekha kwa wansembe, nupereke nsembe ya pa cikonedwe cako, monga adalamulira Mose, kukhale umboni kwa iwo. (Luka 5:14)

KODI ACHITE CHANI NGATI SANACHIRITSIDWE:

Musalore kuti anthu akhumudwe chifukwa sanachiritsidwe. Pewani kupeza chifukwa chomwe chachititsa kuti asachiritsidwe (pokhapokha ngati Mulungu wamvumbulutsa mwapaderadera). Asanayambe kupemphera auzeni popeza sanawone zotsatira ndi maso awo zotsatira izi sizikutanthauza kuti sanachiritsidwe. Machiritso amayambiri ku uzimu. pali machiritso ochedwerapo, monga ngati machiritso akusabereka kwa Abrahamu ndi Sarai, ngakhale kuti Mau anaperekedwa pakalebe.

Komaso nthawi imakhudzidwa. Tamuganizireni munthu wolumala pa chipata chakachisi pa Machitidwe 5. Yesu amkadutsa pachipata chakachisicho nthawi zambiri, koma timauzidwa kuti munthu wolumalayu anakhalapo kwa zaka zambiri. Mmalu mwake anazachiritsidwa ndi Petro ndi Yohane patsogolo (Machitidwe 5:15-16). Panalinso nthawi yoyikika pa nkhani ya Yobu ndi Lazar.

Mwina mukhoza kufuna kuika munthu woti azigwira ntchito yolondola antthu odwala potsatira ndondomeko zotsatirazi:

1. Pitirizanibe kukakamira mupemphero la machiritso: Yesu anaphunzitsa kukakamirabe mupemphero. Iye sanaletse kutero. Itanani akulu ampingo kuti azakupempherereni.
2. Pitirizanibe kumanga chikhulupiriro chanu: Muntha kuchita zimenezi pophunzira “Rhema” Mau a Mulungu amachiritso.
3. Pitirizanibe kumvomereza machimo anu: vomerezani machimo anu tsiku ndi tsiku kuti asawononge thupi lanu. Khalani ndikuyenda mkumvera kwa Mau a Mulungu.
4. Gwiritsani ntchito mphamvu zanu za uzimu: Okhulupirira onse ali ndi maziko a machiritso ndi mamasuridwe. Yambani kuwagwiritsa ntchito. Izi ndi:
 - Mau a Mulungu.
 - Mwazi wa Yesu.
 - Mau a umboni wanu.
 - Ulamuliro womanga kapena kumasula.
 - Pemphero ndi matendo.
 - Zida zakhondo zomwe ziri pa Aefeso 6:10-18.
 - Ulamuliro ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.

5. Ngati pali poyenera, sithani kakhalidwe ka moyo wanu: Chotsani chikhalidwe chonse chauchimo ndi chosayenera. Machiritso amchitika pamene mukukhala mogwirizana ndi kumvera Mau a Mulungu.
6. Tsatirani malangizo a M' malembo a moyo ndi kukhala mwathazi.
7. Khalani pamalo achikhulupiriro: zunguliridwani ndi malo omwe machitachita ake ndi achikhulupiriro pokhala mbali imodzi yamkumano wa okhulupirira.
8. Ziperekeni nokha kwa nthunthu kwa Mulungu: Chikhulupiriro chathunthu chimatanthauza kuti pakukhala moyo kapena kumfa, matenga kapena moyo wanthazi, madziwa kuti muli mmanja mwa Mulungu. Yohane 10:29; Yobu 13:15; 19:26.
9. Khalani odekha pakuzuzika: Pamene mukudikira machiritso amphumphu, khalani modekha pakuzuzika kwanu mu njira yakuti ena azakopeka nawo. Mukhoza kuchita choncho pochita izi:
 - Kuyamika: 1 Atesalonika 5:16-18.
 - Kulola Mulungu kuti awonetsere mphamvu Yake mchifoko: 2 Akorinto 12:9-10.
 - Kukhala odekha pamene mukudikirira. Anthu amadikira zotsatira zazoyezedwa zawo mu ofesi ya dotolo. Timadikira kuti makhwala agwire ntchito. Nchifukwa chani sitimadikira pa Mulungu? Onse amane ali odekha amalandira malonjezano: Ahebri 6:12; 12:2; Yakobo 1:2-4; 5:10-11; Masalimo 27:14; 37:34; Yesaya 40:31; Aroma 5:3-5.
 - Zindikirani kuti palibe kuzuzika kopanda cholinga: werengani zomwe Baibulo linalemba za onse omwe anazuzikapo.
10. Tengani malonjezano a Mulungu: Ngakhale pomwe mukuwona ngati kuti Mulungu wakusiyani, pitirizanibe kukumbutsa malonjezano ndi kupemphera mapemphero awa: Masalimo 5:1-3; 6:2-9; 13:1-6; 22:19; 27:7; 31:21-22; 42:9-11; 54:1-2; 55:1-2; 70:1; 71:9-21; 86:6-7; 94:19; 102:1-7; 2 Akorinto 4:17-18.
11. Patsani ndipo muzalandira: Baibulo limaphunzitsa ndondomeko yofunikira kwambiri yamuufumu wa Mulungu ndiyakuti timalandira pamene tapereka. Ngati ndinu okhulupirira, yambani kutumikira mphamvu yamachiritso a Mulungu kwa ena. Pamene mukupereka, muzalandira.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la machiritso osawonera.

2. Fotokozani chisamaliro chowatsatira onse amene anachiritsidwa.

3. Fotokozani chisamaliro chowatsatira onse amene sanachiritsidwe.

(Mayankho amayesowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Kodi munayambapo mwalandira pemphero kapena kupemphera wina wake ndipo machiritso sanawonekere?

Lembani ndandanda wa zotsatirazi pa ndondomeko iri yonse:

Pitiriranibe kukakamira pamachiritso:

Pitirizanibe kumanga chikhulupiro chanu:

pitirizanibe kumvomereza tchimo lanu:

Gwiritsani ntchito mphamvu zanu za uzimu:

Sithani makhwalidwe anu:

tsatirani ndondomeko za Mmalemba zoti mukhalire moyo wathazi:

Pangani malo achikhulupiro:

Ziperekeni nokha kwathuthu pokhulupirira Mulungu:

Khalani odekha mmavuto:

Funsani malonjezano a Mulungu:

Perekani ndipo muzalandira:

2. Ngati simunalandire machiritso anu, werengani Yohane 11. Nkhani yakuukitsidwa kwa Lazalo imawonetsera kuti machiritso akachedwa amapereka mwayi wowonetsera mphamvu ya Mulungu yopambana.

3. Kodi munayamba mwalandira kapene kupempherapo wina wake amene analandirapo machiritso? Lembani dongosolo lamomwe mungamutsatire machiritsowo:

Zindikirani ziwembu zasatana:

Kanizani ziwembu zasatana:

CHAPUTALA 16

MACHIRITSO OMALIZA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kupereka ndondomeko zapaderadera zotumikirira kwa amene adwalika kwambiri.

LONJEZANO LA MACHIRITSO:

Cifukwa cace sitifoka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku.

Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero;

Popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:16-18)

CHIYAMBI

Baibulo limawonetsera kuti pali nthawi yoyikika yoti munthu wina aliyense azamwalire.

Pakuti copangiratu ciona mphamvu atafa mwini wace; popeza ciribe mphamvu konse pokhala wolemberayo ali ndi moyo. (Ahebri 9:17)

Phunzirani ndondomeko zotsatirazi ngati inu mwadwalika kwambiri ndipo gwiritsani ntchito kuthandizira kutumikira kwa wina amene wadwalika:

KUTUMIKIRA KWA AMENE ADWALIKA KWAMBIRI

1. Pali nthenda yokutengera ku imfa: Pa Yohane 11:4 Yesu anati nthenda ya Lazalo sinali yomutengera ku imfa. Izi zikutathauza kuti pali nthenda zina zomwe zimatengera ku imfa.
2. Pali mitundu iwiri ya imfa yachilengedwe:
 - A. Imfa yobwera mwachangu: Imawononga thupi kuti mzimu ukapulumeke. (1 Akorinto 5:4-5)
 - B. Imfa yololezedwa: Chifukwa chazochitika zazochitika za moyo zachilengwe (Ahebri 9:27; Mlaliki 3:2; 2 Mafumu 13:14; Yesaya 38; 2 Mafumu 20)

3. Cholinga chamachiritso sikutanthauza kuti sitizafanso:
 - A. Ngakhale amene Yesu anawaukitsa kwa akumfa pamapeto Pake anazamwaliranso.
 - B. Anthu ena amasungidwa mwa umulungu kuzotsatira za ukalamba monga momwe analiri Mose. Ena amatsata njira ya chilengedwe yaukalamba, monga momwe analiri Yoswa.
 - C. Baibulo silinalonjeze kusamwalira padziko pano ngati mbali imodzi yapangano lamachiritso. Musazunguzike pamene Khristu amene wakhulupirira ndikulandira machiritso akumwamba kumatenda kenako mkumwalira. Izi zinachitikanso kwa Elisa, koma zaka zambiri mafupa ake anali ndi mphamvu yodzutsa munthu womwalira. Izi zikutathauza kuti sikuti anamwalira chifukwa chosowa chikhulupiro!

4. Pamene mukutumikira kwa munthu wodwalika kwambiri muzifusa nzeru kwa Mulungu: Kodi ino ndi nthawi yoyikika ya munthuyu kuti amwalire?

- A. Ngati Mulungu angabvumbulutse kuti ndi nthawi yoyikika, nde athandizeni kuti akozekere monga ngati mmene Yesu anachitira ndi mbava zija pa mtanda.
 1. Mukhatsimikizike kuti akumudziwa Yesu monga mpulumutsi wawo.
 2. Ngati ali okhulupirira, onetsetsani kuti palibe tchimo limene sanalape.
 3. Alimbikitseni kuti aike zochita zawo mmalo mwake.
 4. Alimbikitseni kukozaso maubale ngati panali mavuto pakati pa iwo ndi anthu ena.
 5. Athandizeni kumvetsetsa kuti imfa imabwera kwa wina aliyense: kwa okhulupirira, imfa mkati mwa moyo wosatha tinali nawo kale. Tikuyenera tisi the mawonedwe anthu. Sitikuyenera kusaka imfa. Kusowa kuthupi ndekuti mkukhala ndi Ambuye (2 Akorinto 5:8). Imfa ndi mdani, ndipo ndi mdani womaliza yemwe azawonongedwe (1 Akorinto 15:26). Kuukitsidwa kwa Yesu chinali “chipatso choyamba” kuwonetsera imfa yagonjetsedwa koma sinawonongedwe. Ndi khondo ya mdaniyi yomwe imawalanda zida okhulupirira (1 Akorinto 15:55).
 6. Athandizeni kumvetsetsa kuti Mulungu ndi wamphamvu zonse. Akhonza kulowerera nthawi ina iliyonse mkuwapangitsa iwo kuti akhale ndi moyo wautali.
 7. Akumbutseni iwo kuti imfa ndi machiritso omaliza. Sipamakhalanso ululu uliwonse kapenaso kudwala. Timalowa mkupezeka kwa Mulungu mwamphumphu. Kudwala kuli ngati tchimo. Tinapulumsidwa kuchilango cha tchimo (kudwala) pamene tinalandira Yesu kukhala Mpulumutsi ndi Mchiritisi.

Tikhoza kupitirirabe kumasulidwa kumphamvu yake monga ngati okhulupirira, koma mtsogolo pamene tizapite kukhala ndi Ambuye. Mulungu ali ndi njira yotembenuza zinthu zomwe satana anazikonza kuti zikhale zoipa koma Iye amazisitha mkukhala zabwino. Imfa chinali chilango cha tchimo, koma chifukwa cha imfa Yesu inabweretsa moyo. Ichi nchifukwa chake imfa inamezedwa nchigonjetso. Mu imfa, Mulungu amabweretsa machiritso amuyaya.

8. Aike chidwi chawo pa moyo wamuyaya ndi chiukitso. Gwiritsani malemba otsatirawa: Yohane 11:5-6; Yobu 19:25-27; Aroma 8:10-11, 17-18, 22-23; 10:11; 1 Akorinto 15:42-44, 54-58; 2 Akorinto 4:16-18; 5:1; 1 Atesalonika 4:13-18.

B. Ngati simunalandire Rhemah mau a Mulungu ngati iyi iridi nthawi yake yoyikika ya imfa.

1. Pitirizani kupempherera machiritso molingana ndi chifuniro cha Mulungu. Izi sizifuna njira zanthu, koma kumulola Mulungu kuti achite malingana ndi chifuniro Chake, kuti kaya awatenga iwo kapena azawaukitsa. Mkofunikaso kupemphera mu Uzimu, popeza Mzimu Woyera amadziwa chifuniro cha Mulungu ndipo azapemphembedzera moyenerera (Aroma 8:26).
2. Alimbikitseni odwala kuti azipereke okha kuthuthu pokhulupirira Mulungu, kaya pokhala ndi moyo kapena pakumwalira. Yohane 10:29; Yobu 13:15.
3. Pempherani mu Uzimu, popeza Mzimu Woyera amadziwa chifuniro cha Mulungu ndipo amapemphembedzera moyenerera (Aroma 8:26).
4. Ikachi chidwi pa utumiki okozekera imfa ngakhaleso machiritso akuthupi.
5. Imfa ndi machiritso omaliza: kwa okhulupirira, imfa ndimachiritso omaliza. Sikuzakhalaso ululu kapena kudwala ndipo muzalowa mukupezeka kwa Mulungu muli woyeretsedwa. Nthenda ndi tchimo ndizofanana: Tinapulumsidwa kuchilango cha tchimo (nthenda) pamene tinalandira Yesu momga Mpulumutsi ndi tchiritsi, komandi mtsogolo mokha pamen tizapite kukhala ndi Ambuye ndipamene tizapulumsidwe mkukupezeka kwawo.

Mulungu ali ndi njira yogwiritsa ntchito zinthu zimene satana analinazomalingaliro oipa. Imfa inali chilango cha tchimo, ndipo chifukwa cha imfa ya Kristu moyo unabwera. Ichi nchifukwa chake imfa inamizidwa muchigonjetso chifukwa onse amene anamfa iri mwa Kristu azaukaso.

Taonani, ndikuuzani cinsinsi; sitidzagona tonse, koma tonse tidzasandulika, m'kamphindi, m'kutwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osabvunda, ndipoife tidzasandulika.

Pakuti cobvunda ici ciyenera kubvala cisabvundi, ndi caimfa ici kubvala cosafa. Ndipo pamene cobvunda ici cikadzabvala cisabvundi ndi caimfa ici cikadzabvala cosafa, pamene padzacicitika mau olembedwa, Imfayo yamezedwa m'cigonjetso.

Imfawe, cigonjetso cako ciri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti? (Akorinto 15:51-55)

Pamene wokhulupirira wamwalira, tikuyenera kukondwera chifukwa chinthu chantengo wapatali chachitika:

Imfa ya okonedwa ace Nja mtengo wace pamaso pa Yehova. (Masalmo 116:15)

Kwa wokhulupirira, imfa imabwera monga ngati kumasulidwa kuchoka kudziko lauchimori:

Pakuti tidziwa kuti ngati nyumba ya pansi pano ya msasa wathu ipasuka, tiri naco cimango ca kwa Mulungu, ndiyo nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha, m'Mwamba. Pakutinso m'menemo tibuula, ndi kukhumbitsa kubvekedwa ndi cokhalamo cathu cocokera Kumwamba; Pakutinso ife okhala mu msasawu tibuula, pothodwa; si kunena kuti tifuna kubvulidwa, koma kubvekedwa, kuti caimfacu cimezedwe ndi moyo. (Akorinto 5:1-2,4)

Pa imfa, wokhulupirira amalowa mukupezeka kwa Mulungu:

koma tilimbika mtima, ndipo tikondwera makamaka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye. (2 Akorinto 5:8)

Muntu wina dzina lake Brisbane anaifanizra malira awokhulupirira monga ngati gulu la athu okhumudwa akatapila omwe onse amvala ma suti akuda, amene akulira ngati anyamula gulugufe kukamuika kumalo ake otsiriza. Pamwamba pawo pali maluwa okongola kwambiri ngati gulugufe.

KUCHITA MAWU

1. Onani lonjezano lamachiritso mu phunziro lino:

Cifukwa cace sitifoka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku. Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero; popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. Ngati munatumikirapo kapena mukutumikira kwa wina wake amene wadwalika Zambiri, funsani mafunso awa: (2 Akorinto 4:16-18)

Kodi nyengo iyi ikukuchititsani kuti muzikomoka ku uzimu?

kodi munthu wanu wamkati akumatsitsitsidwa tsiku ndi tsiku, kusatengera nyengo zimene munthu alomo?

Kodi mungakozenso bwanji munthu wanu wamkati?

Kodi chidwi chanu mukuyika pa zinthu zimene zinakali zakanthawi kapena zamuyaya?

2. Ngati mukutumikira kwa munthu yemwe wadwalika kwambiri ndipo Mulungu wawonetsera kuti munthuyu nthawi yake yoyikira kuti amwalire yafika, gwiritsani ntchito njira izi: Kodi mumamudziwa Yesu ngati Mpulumutsi?

Ngati muli wokhulupirira, kodi muli ndi tchimo lomwe simunalape? Pempherani chifukwa chatchimo losalapa, monga ngati mkwiyo, kuwawidwa mtima, ndizina zotero. Mvomerezani ndi kulandira chikhululukiro (1 Yohane 1-8-9).

Kodi mwaika zinthu zanu mchimake? Ngati ayi, lembani zinthu zimene mukufuna kuti muchite:

Kodi pali ena amene mukufuna kuti muyanjane nawoso, kupempha chikhululukiro, kapena kuthana ndi zovuta? Ngati ndi choncho, lembani maina awo mmusimu:

3. Ngati simunalandire chidziwitso chochokera kwa Mulungu kuti ngati iridi nthawi yoyikika yomwalira, tsatirani ndandanda uwu:

- Pitirizanibe kupempherera machiritso malingana mwachifuniro cha Mulungu.
- Kupemphera mu Uzimu chifukwa amadziwa chifuniro cha Mulungu ndipo amapembedzera moyenerera.
- Alimbikitseni odwala kuti azipereke kwathuthu pokhulupirira Mulungu, ndicholinga chakuti kaya pokhala ndi moyo kaya pakufa, akuyenera kuzindikira kuti ali mdzanja la Mulungu.

4. Ngati inu, kapena wina wake amene mukutumikira, akudwalika kwambiri, funsani lonjezano iri:

Ndipo Yesu anawayang'ana, nati kwa iwo, ici sicitheka ndi anthu, koma zinthu zonse zitheka ndi Mulungu. (Mateyu 19:26)

5. Nthawi zonse kumbukirani kuti Mulungu ndi wamphamvu, ngakhale kuti munthuyu wauzidwa kuti akudwalika, Akhoza kulowerelapo pa nthawi ina iriyonse ndikutalikitsa moyo wawo. Werengani nkhani ya mfumu Hezekiya pa Yesaya 37:1 kufikira 38:22. Pamene Hezekiya amkamwalira, anatembenukira kwa Mulungu ndipo analandira machiritso. Muzochitikazi awona zinthu izi:

- | | |
|-------------|----------------|
| - Ugwiro | Yesaya 38:1 |
| - Pemphero | Yesaya 38:2-3 |
| - Lonjezano | Yesaya 38:4-6 |
| - Kutamanda | Yesaya 38:9-20 |

GAWO LACHISANU NDI CHIMODZI

NDONDOMEKO ZA MAMASULIDWE

Mugawo lino muphonzira ndondomeko zotumikirira ndi kulandira mamasulidwe. Muphonzira zokhudzana:

- **KODI NDINDANI AMENE SATANA WAMUMANGA.**
- **KUTUMIKIRA MAMASULIDWE.**
- **UTUMIKI WOLONDOLA WAMAMASULIDWE.**

CHAPUTALA 17

AMENE SATANA WAMUMANGA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO wosawonera.
- Kuwonetsera magawo atatu akuluakulu amitundu ya ziwanda zomwe zimachitira chiwembu thupi, moyo, ndi mzimu wa munthu.
- Kufotokoza kufunika kwa mphatso ya chidziwitso pothana ndi mphamvu ya ziwanda.
- Kufotokoza tanthauzo la mau oti kuponderezedwa ndi ziwanda.
- Kuwonetsera makhalidwe a munthu amene akuponderezedwa ndi ziwanda.
- Kufotokoza tanthauzo mau oti kuzuzidwa ndi ziwanda.
- Kuwonetsera makhalidwe amunthu amene akuzuzidwa ndi ziwanda.
- Kufotokoza mmene ziwanda zimatengera ulamuliro.

LONJEZANO LAMACHIRITSO:

Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

CHIYAMBI

Kwanthawi yayitali ntchito ya ziwanda yakhala ikutsutsidwa ndi anthu ambiri kukhala machitachita achikhalibe achikunja. Sizinatengwe kukhala mvuto lomwe limalowa miyoyo, makomo, makachisi, ndi maiko. Koma anthu ngati inu omwe akuzuzidwa, kuvutitsidwa, ingakhalenso kulowedwa ndi mphamvu yakumidima yomwe imadziwika kuti ziwanda. Yesu anatomikira kwa onse amene anakhudziwa andi mphamvu ya ziwanda (Machitidwe 10:38) ndipo analamula omutsatira Ake kukachita chimodzi modzi pamene amkafalitsa Uthenga Wabwino wa Ufumu (Mateyu 10:1).

Chaputala chino chikuwonetsera ndondomeko zakutumikira kwa onse omwe akhudziwa ndi mphamvu ya ziwanda. Kuti akalandire Uthenga Wabwino akapolo amenewa koyambirira akuyenera kumasulidwa kumsingazo. (Sukulu ya Harvest Internation iri ndi phunziro lotchedwa “Ndondomeko za Uzimu: *Buku la nkhondo ya Uzimu*: lomwe limapereka ndondomeko wa machitachita a satana ndi mphamvu ya ziwanda. Ngati simukudziwa za nkhondo ya uzimu, mukuyenera kupeza buku limenero musanayambe utumiki wamamasuridwe.

YESU NDI ZIWANDA

Kuphunzitsa ndi utumiki wa Yesu unawonetsera kuti mizimu yaziwanda ndi mphamvu yazoipa zeni zeni. Zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana ndi ziwanda ndi momwe anathanirana nazo zimapereka uthenga wamachitachita a satana.

Yesu anamvomereza kuti satana ndi olamulira wa ziwanda. Anaphunzitsa zowona zake za mphamvu ya ziwanda. Iye anati kutulutsa ziwanda ndi chizinfikiro chimodzi chosonyeza kuti Ufumu wa Mulungu wabwera. (Werengani Mateyu 12:22-30, Marko 3:22-27, ndi Luka 11:14-23 pachidule cha zomwe Yesu anaphunzitsa zokhudzana ndi ziwanda.)

Mbali yayikulu ya utumiki wa Yesu unakhudza pothana ndi ziwanda. Ndi chitsanzo cha Yesu ndi ulamuliro wa dzina Lake omwe umapereka maziko a Malemba othanirana ndi mphamvu ya ziwanda. Yesu anatomikira kwa onse omwe anabwera ndi mvuto laziwanda:

...Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

Pa “zoonjezera kuphunzira” mbali ya phunziro lino muphunzira zolembedwa zapaderadera za m’Baibulo pomwe Yesu anathanirana ndi mphamvu ya ziwanda.

MMENE ZIWANDA ZIMAGWIRIRA NTCHITO

Ziwanda zimagwiritsidwa ntchito ndi satana kutsutsana ndi Mulungu, zolinga Zake ndi anthu Ake. Amamenyaso nkhondo ndi anthu osakhulupirira kuti asadziwe choonadi cha Uthenga Wabwino. Ziwanda zimatenga ulamuliro wadera lina (maulamuliro) monga ngati kalonga waku Perezani yemwe anatchulidwa mu Daniel 10:12-13. Ziwanda zimagwiranso ntchito kupyolera mpakukhala ngati anthu, mwa amuna ndi akazi, pokakwaniritsa zolinga za satana pa dziko.

Kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu nde cholinga chachikulu chasatana. Mau oti “satana” matanthauza kuti “mdani.” Satana ndi mdani woyamba wa Mulungu (Yobu 1:6; Mateyu 13:39). Munthu ndi mdani wake wachiwiri (Zakariya 3:1; 1 Petro 5:8).

Ziwanda ziri ndi mawonekedwe osiyanasiyana. Chiwanda china chinazifotokoza chokha mu 1 Mafumu 22:23 monga ngati mzimu wabodza. Mzimu wosamva ndi wosayakhula unatchulidwa mu Marko 9:25. Ziwanda zamawonekedwew osiyanasiyana zimagwira ntchito ngati mizimu yobweretsa zowawa, mizimu yopangitsa chigololo, ndi mizimu yonyasa. Satana amazigwiritsa ntchito polimbana ndi munthu kuthupi, moyo ndi mzimu.

MIZIMU YA ZIFOOKO:

Iyi ndi mizimu imene imazuza matupi a anthu okhulupirira ngakhalenso osakhulupirira. Werengani Luka 13:10-17. Mzimayi ameneyu anazuzidwa ndi mzimu wa zofoka. Anapezeka pa tsiku la sabata ndi Yesu anamuitan iye kuti “mwana wamkazi wa Abrahamu.” Mfundo zonsezi zikuwonetsa kuti iye anali wotsatira Mulungu, koma thupi lake linazuzidwa ndi satana kwa zaka zisanu ndi zitatu. (Zitsanao zina za mphamvu ya ziwanda yomwe imazuza thupi onani Mateyu 12:22; 17:15-18; Machiritso 10:38; 2 Akorinto 12:7.)

MIZIMU YOKOPA PONYENGERERA:

Mizimu imeneyi imazuza mzimu wa munthu, kumukopa iye kuti akhulupirire chiphunzitso chonama, kuti akalandire chilango chosatha kumapeto kwake. Ndimizimu yaziphunzitso chonyenga, Akhiristu onama ndi aphunzitsi onyenga:

Koma Mzimu anena monenetsa, kuti m' masiku otsiriza ena adzataya cikhulupiriro, ndi kusamala mizimu yosoceretsa ndi maphunziro a ziwanda. (1 Timoteo 4:1)

Pakuti ali mizimu ya ziwanda zakucita zizindikilo; zimene zituruka kumka kwa mafumu a dziko lonse, kuwasonkhanitsira ku nkondo ya tsiku lalikuru la Mulungu, Wamphamvuyonse. (Cibvumbulutso 16:14)

Ndiye amene kudza kwace kuli monga mwa macitidwe a Satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikilo ndi zozizwa zonama.

Ndi m'cinyengo conse ca cosalungama kwa iwo akuonongeka, popeza cikondi ca coonadi sanacisandira, kuti akapulumsidwe iwo. (2 Atesalonika 2:9-10)

Mizimu yokopa mkuphatikizapo mzimu wa zamaula omwe unatchulidwa pa Machitidwe:

Ndipo panali, pamene tinalinkunka kukapemphera, anakomana ndi ife namwali wina amene anali ndi mzimu wambwebwe, amene anapindulira ambuye ace zambiri pakubwebweta pace. (Macitidwe 16:16)

Mizimu yamaulayi kapena “mizimu yachizolowezi” imagwira ntchito mwa amaula, amfiti, ndi owombeza ndi anyanga. Kupyolera munjira yosakhala yammalemba mizimu yam aula imatha kunena zakutsogolo kapena kuzindikira nzeru zomwe zimadziwika mwachilengedwe. Machenjezo okhudzana ndi mizimu yachizolowezi aperekedwa pa Levitiko 19:31; 20:6; Deutoronome 5:9; 18:10; Levitiko 20:7; ndi 1 Samueli 28:3.

Mizimu yonyengerera imatha kuwona chikumbumtima, kukopa, kunyengerera, kuika chidwi, kusangalatsa, kumutsa mudyo, kukopa, ndi kunyenga. Mizimu yonyengerera ndi yachangu pochititsa “kuika kwa uzimu mmalo akuluakulu.” Nthawi zonse imakhalapo ndipo imagwira ntchito zipembedzo zokana Yesu ndi paliponse pamene chiphunzitso chonyenga chikuchitika. Kumbukirani kuti satana amafuana kulambiridwa ndipo akhoza kutenga kulikonse komwe angawapeze. Mizimu yokoka imanyengerera amuna ndi akazi kuti azilambira mafano ngakhalesnso satana amene.

MIZIMU YONYANSA:

Mphamvu yaziwandayi imazuza moyo wa munthu. Imakhudzidwa ndi makhalidwe achigololo, maganizo onyasa, kusaupeza mtima ndi machitachita ena ausatana omwe amagwiritsidwa ntchito kumanga amuna ndi akazi. Pamene satana akumulamulira munthu ndi mizimu yonyasa, amagwirisa ntchito mmakomo, makachisi, ndi padziko lonse popeza malo onsewa makhala

anthu. Umu ndi mmene satana amagwirira ntchito madela osiyanasiyana. Zitsanzo za mizimu yonyasa onani Mateyu 10:1; 12:43; ndi Mark 1:23-26.

KUPONDEREZA, KULALAMULILIDWA, KULOWEDWA

Mizimu yoyipa imatha kumapondereza anthu. Kupondereza kumatanthauza kuti kukakhali pansu, kulimbana, kapena kukutsekera kunjira. Kupondereza kumeneku kumatsatana ndi mizimu yoyipa mu njira zambiri. Imabweretsa kukhumudwa, imapanga nyengo zonyasa, ndipo imapereka malingaliro oipa monga maganizo ofuna kuzipha, chigololo, kusakhulupirira, matha, ndi zina zambiri. Ziwanda zimalenga machitachita awusatana.

Za Yesu wa ku Nazarete, kuti Mulungu anamdzoza iye ndi Mzimu Woyera ndi mphamvu; amene anapitapita nacita zabwino, naciritsa onse osautsidwa ndi mdierekezi, pakuti Mulungu anali pamodzi ndi iye. (Macitidwe 10:38)

Ziwanda zimatha kulowaso anthu. Kulowedwa ndi ziwanda ndi nyengo imene chiwanda ndi nyengo imene mizimu yoyipa (ziwanda) zimalowa ndi kumakhal mu thupi la munthu ndipo zimatenga ulamuliro wamunthuyo kwanthuthu konse. Anthu ena amakonda kugwiritsa ntchito mau akuti “kulumulidwa ndi ziwanda” osati kugwidwa ndi ziwanda, koma mosataterenga dzina lomwe likugwiritsidwa ntchito, munthu wolowedwa ndi ziwanda ndi yemwe amakhala nyumba yokhalamo ziwanda. “Kulowedwa” sizikutanthauza kuti munthu alibe udindo pamachimo ake. Udindo wake ndi umene wachititsa kuti allowedwe ndi ziwanda.

Kulowedwa kukhoza kuchita mochita kufuna. Munthu antha kufuna kulowedwa ndi mphamvu ya mizimu ndicholinga chakuti azitha kuwona zakutsogolo, kutemberera, kuti akhale mfiti, komaso kuti akhale ndi mphamvu zodabwitsa. Kulowedwa kukhozaso kuchitika mosafuna. Munthu oti sanafune kuti allowedwe, koma kupyolera mmalingaliro awuchimo, machitidwe, kapena kuyanjana ndi anthu aziwanda kukhoza kumpangitsa munthu kuti allowedwe ndi ziwanda.

Mphamvu ya ziwanda imagwira ntchito mwamakolo ndipo machimo amakolo atha kukhudza m'bado winawo (Onani Eksodo 20:5; 34:7; ndi Deutoronome 5:9). Izi zikukamba za kulowedwa ndi ziwanda kapena kuponderezedwa kwa ana monga momwe zinalmbedwera pa Marko 7:24-30 ndi 9:17-21.

KODI ZIWANDA ZIMAKHUDZANSO OKHULUPIRIRA?

Okhulupirira weniweni sangalowedwe ndi ziwanda chifukwa Mzimu Woyera sungakhale mu kachisi chimodzi ndi mzimu woyipa.

Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu?

Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wapatali; cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu. (1 Akorinto 6:19-20)

Pamene uli wakwa Mulungu ndipo wadzadzidwa ndi Mzimu Woyera, sungakhale wasanatana mkudzadzidwaso ndi mizimu yake pa nthawi imodzi. Mzimu Woyera sangakhale pamalo amodzi mkachisi imodzi ndi satana.

Koma izi sizikutanthauza kuti okhulupirira sangakhudzidwe ndi mphamvu ya ziwanda. Ndi mphamvu yomweyi imene timakhala tikulimbana nayo. Satana amagwiritsa ntchito mphamvu ya ziwanda pochitira ziwembu okhulupirira kuchokera kuja popyolera kuwapondereza, zizindikiro za zimenezi zinakambidwa kale pambuyo. Koma sizingalowe mwa okhulupirira weni weni. “Kulowedwa” kumawonetsa kukhazikika mkati. “Kupondereza” kumasonyeza zochochela kunja. Machitachita a okhulupirira akhoza kukhala ausatana ngati angalole kuti mphamvu ya ziwanda iwapondereze. Kuponderezedwa kotereku ndi mphamvu yoyipa kumampatsa mpata satana kuti awagwiritse ntchito pa zolinga zoyipa.

Izi ndi zomwe zinachitika pamene Petro, ophunzira wa Yesu, anagwiritsidwa ntchito ndi satana pofuna kumuletsa Yesu kukamva zowawa chifukwa cha machimo a anthu onse. Pamene Yesu ananena za mazunzo amene azakumane nawo, Petro anati:

...Dzicitireni cifundo, Ambuye; sicidzatero kwa Inu ai. (Mateyu 16:22)

Yesu anati kwa Peturo

...Pita kumbuyo kwanga, Satana iwe; ndiwe condikhumudwitsa Ine; cifukwa sumasamalira za Mulungu, koma za anthu. (Mateyu 16:23)

Sikuti Yesu amkatanthauza kuti Petro ndi satana. Anazindikira kuti pa nthawi imeneyo Petro anamulola satana kuti agwire ntchito kupyolera mwa iye. Sikuti analowedwa ndi ziwanda, koma analola kuti mizimu ya satana kuti imugwiritse ntchito. Kupyolera mu zochita zawo, okhulupirira “amampatsa mpata” (kupereka mwayi) kwa satana kuti awagwiritse ntchito (Aefeso 4:27)

Pamene munthu wabadwanso mwatsopano, dzina lake limalembedwa mu buku lapaderadera ku Mwamba lomwe limatchulidwa kuti buku la moyo. Okhawo amene maina awo ali m’buku limeneri ndamene adzakakhale Kwamwamba kwa muyaya:

Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto. (Cibvumbulutso 20:15)

Zoteka dzina lanu kulembedwa m’buku lamoyo, koma keneko mkufufutidwamo chifukwa chobwerera ku moyo wauchimo:

koma 4 ndipumpuatha thupi langa, ndipo ndiliyesa capolo; kuti, kapena ngakhale ndalalikira kwa ena, ndingakhale votayika ndekha. (1 Akorinto 9:27)

Paulo anazindikira kuti tchimo. makamaka machimo osalapa akuthupi, kukhoza kuchititsa kuluzwa moyo wake womwe ngakhale analalikira kwa ena.

Popitiriza kukhalabe mu uchimo kumachititsa kumapangitsa kubwerera mbuyo. Izi zikutanthauza kuti simakhalanso okhulupirira Yesu Khristu weni weni. Ngati mupitirizabe kumachimwacew mwadala ndi kusamalapa, palibe amene azakuzuni kuti malekera pati kukhala otsatira wa Yesu ndipo makhalano mbali imodzi ya ufumu wa satana. Ndi Mulungu yekha amene angadziwe malire anu. Koma zimenezi zikachitika, makhala kuti mwatsegula nokha nkhomo kwa mdaniyo, kuphatikizapo kupereka mwayi oti ziwanda zikuloweni. Ndi chifukwa chake kuli kofunika kwambiri kuti mukachimwa muzilapa mkubwereranso kunjira yachiyero:

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. Tikanena kutisitidacimwa, timuyesa iye wonama, ndipo mau ace sakhala mwa ife. (1 Yohane 1:9-10)

Yesu amatchulidwa kuti Mau a Mulungu mmalo ambiri m'malemba. Ngati Mau a Mulungu sakhala mwa inu, ndekutiso Yesu sakhala mwainu.

MMENE ZIWANDA ZIMATENGERA ULAMULIRO

Ziwanda zimatenga ulamuliro munjira zambiri:

- 1. Kupyolera kumibado:** Ziwanda zikhoza kupondereza kapena kumulowa munthu chifukwa cha chakulowedwa ndi kuponderedwa kwa makolo kalelo. Izi zimapangitsa kuti ziwanda zizigwiranso ntchito mwa ana (Eksodo 20:5; 34:7; Deutoronome 5:9).
- 2. Kupyolera malingaliro:** Mmalingaliro ndi malo amodzi akulu amene asatana amakondamo kumenenya nkhondo. Ngati satana angalamulire maganizo anu, mapeto ake azatenganso ulamuliro wazochita zanu. Kusowa koteteza malingaliro anu kuzapangitsa kuti muzilephera kukganiza bwino komwe kumapangitsa kuti muzingochita uchimo. Kupitiriza kumangochimwa mmaganizo ndi muzochita kukhoza kupangitsa kuti muponderezedwe komaso mulowedwe ndipo pamapeto pake muzakhala ndi maganizo ozunguzika monga mowe amanenera pa Aroma 1. Awa ndi maganizo amene akugwiritsidwa ntchito ndi satana. ziwanda zimapezaso danga kupyolera mmalingaliro kupyolera kuika makhwala ozunguza bongo amene amachepetsa kaganizidwe kokaniza ziwanda ndipo zimakhala ndi mwayi wolowa kwambiri.
- 3. Kupyolera machitachita auchimo:** Maganizo auchimo posakhalitsa amadzadzidwa ndi machitachita auchimo. Mwachitsanzo, maganizo achigololo amakwaniritsidwa pokachitadi chigololocho. Tchimo ndikuwukira, ndipo ndimaganizo owukira ndipo machitamachita ake amaperaka mwayi oti machitachita aziwanda alowere.

Osakhulupirira amene akukhala mu uchimo amatsegula khomo osati kwa kupondereza kokha kwa mphamvu ya ziwanda, komaso kulowedwa. Pakhondo ya uzimu palibe yemwe amangokhala osatenga nawo mbali. Makhala kuti muli kumbali yabwino kapoena

yoyipa. Makhala wakwa Mulungu kapena kwa satana. Ngati muli wa satana ndipo simunabadweso mwatsopano mwa Yesu Khristu, ndekuti ndinu wake kuti akugwiritseni ntchito, kuponderezedwa, kapena kulowedwa monga momwe afunira.

4. **Kupyolera kufuna:** Anthu ena amachita kufuna kukhala pansu pa ulamuliro wa mphamvu ya ziwanda. Amachita izi ndi zolinga zokhala ndi ndimphamvu zoopsyasochitira zinthu zoopsyaso.
5. **Kupyolera mu nyumba yopanda anthu:** Ziwanda zimayensa thupi la munthu mokhalamo mwawo (Mateyu 12:44). Pamene amunthu wamasulidwa ku mphamvu ya ziwanda ndipo sanadzadze nyumba yake ya uzimu pokhala wobadwaso mwatsopano ndi kulandiranso Mzimu Woyera, kulowedwa kukhoza kuchitikaso.
6. **Kupyolera kupatsidwa chilolezo:** Nthawi zina Mulungu amapereka chilolezo ku mphamvu ya ziwanda kuti akakwaniritse zolinga zake zapaderadera. Izi zikhoza kuloledwa kuti kukhala ngati mayesero kwa okhulupirira monga mmene zinaliri ndi Yobu. Zikhozasa kukha; la chiweruzo cha tchimo monga mmene zinaliri ndi mfumu Sauli.

NDINDANI AMENE ANGATHANE NDI MPHAMVU YA ZIWANDA?

Kuthana ndi mphamvu ya ziwanda sintchito yowasiyira atumiki otchuka. Yesu anati okhulupirira onse alimkuthekera kugonjetsa mphamvu ya ziwanda:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda... (Marko 16:17)

Yesu anawapatsa omutsatira Ake kuthekera kothana ndi mphamvu ya ziwanda. Koyambirira anapereka mphamvu imeneyi kwa ophunzira Ake:

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

Koma andilambira Ine kwacabe, Ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu. (Buku Lopatulika 1992)

Anaperekaso mphamvu yomweyo kwa okhulupirira onse:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda... (Marko 16:17)

Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)

Palibe maziko a m’Baibulo oti mkukhulupirira kuti Mulungu amafuna kuti utumiki ofunikawu ungokhala kwa gulu lina la anthu. Munthu wamba wotchulidwa kuti Filipino anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kutulutsa mizimu yoipa ku Samariya (Machitidwe 8). Komai izi sizikutanthauza kuti okhulupirira akuyenera kuthamanga polimbana ndi mphamvu ya ziwanda popanda kukozeke koyenera, monga momwe ana a Skeva anaziwonera (Machitidwe 19).

Mkufunika kwambiri kuti okhulupirira kuti asamatengeke ndiziwanda. Sitinaitanidwekuti tikazame pa ziwanda. Palibe mphatso ya uzimu yo “tulutsira ziwanda.” Koma simukuyera kuwopa mphamvu ya ziwanda. Pamene mwakumana ndi onse amene agwidwa ndi ziwanda, muli ndi mphamvu yobweretsa mamasuridwe ochokera kwa Mulungu.

KUZINDIKIRA KUPEZEKA KWA ZIWANDA.

Pofuna kugonjetsa mphamvu ya ziwanda, mkoyenera kuzindikira kaye kupezeka kwawo ndi ndale zomwe zimagwiritsa ntchito. Mizimu Woyera wapereka mphamvu ya uzimu yapaderadera yotchedwa “kuzindikira mizimu” (1 Akorinto 12:10).

Kuzindikira kumatanthauza kuti “kubvumbulutsa, kusathula, ndi kusiyantsa. Mphatso yozindikira mizimu imamphangitsa okhulupirira kukazindikira mizimu imene ikugwira ntchito mwa anthu. Imamulola iye kukazindikira, kusathula, ndi kuloza mizimu yoyipa.

Mphatso yozindikira mizimu ndiyofunika kwambiri polimbana ndi mphamvu ya ziwanda. Imakupangitsani kuti mukazindikire mwachangu ngati munthu ali ndi mizimu yoyipa kapene ayi. Imaleta kunyengedwa pokopedwa kapena kumizimu yonama. Munthu yemwe ali ndi mphatso imeneyi antha kuzindikira machitachita oipa ndi malingalilo a mohamvu ya ziwanda.

Mwachitsanzo, kusayakhula ndi kusamva kwina (malingana ndizolemba za Baibulo) kumachita ndi mizimu. Kuyakhula ndi kusamva kwina kumakhala zotsatira za ngozi kapene akudwalika. Kuzindikira kumapangitsa kuti mukazindikire choyambitsa chabvutolo komwe kumapereka utumiki wapadera dera.

Sikuti okhulupirira onse ali ndi mphamvu imeneyi yakuzindikira mizimuyi. Ngati okhulupirira alibe mphatso imeneyi pali zizindikiro zakupezeka kwa ziwanda zomwe zingaoneke. Pamene mkazi waku Sumuliko anabwera kwa Yesu mkumpempha Iye kuti amutulutse mwana wake mzimu wonyasa, anati “Mwana wanga wamkazi akuzuzidwa ndi chiwanda” (Mateyu 15:22). Nde anadziwa bwanji izi? Anadziwa izi chifukwa chazizindikiro.

Izi ndi zina mwa zizindikiro zamachitachita a ziwanda:

Kuloweda ndiziwanda kumazindikiridwa chifukwa chakusakhazizika ndi zachilendo za ziwanda, satana, kapena zanyanga. Munthu otereyo amatha kuzama mumachitachita azamatsenga ndipo nthawi zonse amapereka ulemu kwa satana kapena ziwanda, kapena amakonda nthawi yake yambiri amakonda kuphunzira mau a satana.

Kuponderezedwa ndi ziwanda: Kukhoza kuzindikirika ndizizindikiro zotsatirazi:

1. Kumangidwa kwa kuthupi: “Mwana wa mkazi wa Abrahamu” amene Yesu abvumbulutsa mzimu wozuzidwa anamangidwa kuthupi. Onani Luka 13:10-17. Matenda okhalitsa akhoza kukhala kuponderedwa ndi ziwanda. Matenda onse sikuti amabwera chifukwa cha mphmvu ya ziwanda. Matenda ena amayamba chifukwa chophwanya malamulo achilengedwe, monga ngati kusadya kosayenera kapena kumwa madzi kolakwika. Matenda ena chimakhala kuti ndi chikwapu. Mfumu ina m’Bainulo imene sinapereke ulemu kwa Mulungu inakathidwa ndi matenda anjoka za mmimba ndipo mapeto ake inamwalira.
2. **Kuponderezedwa kwa ubongo:** Kusokenekera mmaganizo kapena moyo monga ngati kuzuzidwa kwa maganizo, kuzunguzika, kukaika, kudwala matenda oiywayiwa ndi ena otero. Kusowa mtendere, kusakwanitsa kuganiza bwino kapena kumvetsera kwa ena, kuyakhula zopanda pake. Mavuto onse amubongo sikuti amayambitsidwa ndi satana. Kufooketsedwa, kuponderezedwa, kusokonekera zikhoza kuyamba chifukwa chodana ndi chakudya china kapena kusakaniza kwa makhwala kolakwika mu ubongo. Mulungu ndiothekera kuchiza mavuto amubongo ndi matenda amene samabwera chifukwa cha mphamvu ya ziwanda komaso ngakhale kubweretsa mamasulidwe pamene ngati abwera ndi ziwanda. Koma tikuyenera kukhala osamalitsa osati kupereka matenda onse kapena mavuto aubongo kuti amayambitsidwa ndi mizimu ya ziwanda. Nthawi zina kusitha kophweka pachakudya ndi machitidwe a moyo kukhoza kuchotsa mvuto ngati layamba chifukwa chakusokonekera kwa thupi.
3. Mamvuto amaganizo: Kusokonekera maganizo komwe kumakhalitsa kapena kumazachitikaso, kuphatikizapo kukhumudwa, udani, mkwiyo, matha, kuzivera chisoni, nsanje, kudera khawa, kumva kuti suli otetezeka, kukanidwa ndizita zotero.
4. Mavuto auzimu: Kukhala kuvuta kwambiri kufuna kugonjetsa tchimo, monga ngati chikhalidwe chauchimo. Kukanizidwa kwa yankho la uzimu kumavuto. Mtundu wina uliwonse wa chiphunzitso chonyenga kapena kunyengedwa, kuphatikizapo kumangidwa ku nsinga waziphunzitso za satana.
5. Zochitika: ziwanda zitha kulenga nyengo yovuta yomwe ndi yopondereza. Nyengo imeneyo kawirikawiri imakhudzana ndi chisokonezo ndipo imatha kuzindikiridwa kuti ndi yaziwanda chifukwa Mulungu siamene amayambitsa chisokonezo (1 Akorinto 14:33; Yakobo 3:16).

Kugwidwa ndi ziwanda kukhoza kuzindikirika ndi zizindikiro zotsatirazi:

1. Kudzadzidwa ndi mizimu yonyasa: Izi zimawonetseredwa pochita makhalidwe onyasa. Zikhoza kuphatikizapo kufuna kuyenda opanda zovala. Mwachitsanzo onani Marko 5:2 ndi Luka 8:27.

2. Kukhala ndi mphamvu zodabwitsa: Munthu amawonetsa mphamvu zopitirira muyeso. Mwachitsanzo onani Marko 5:3 ndi Luka 8:29.
3. Kumangozichekacheka: Kuzicheka kumeneku kumatha kutsaganaso ndikutuluka thovu mkamwa. Onani Marko 9:14-29 ndi Luka 8:26-39.
4. Kutsutsa ku zinthu za uzimu: Munkhani ya Pa Marko 6:7 ndi 1:21-28, ziwanda zinamudziwa Yesu ndi masangasanga zinamuza Yesu kuti ziwachokere. Kuopedwa kwa dzina la Yesu, pemphero ndi Mau ndi kunyoza ndizina zonse zomwe ziri za uzimu ndi chizindikiro chakuti munthuyu ali ndi ziwanda. Kunyoza kopitiriza muyezo kukhoza kuzindikirika ndipo kumalamuliridwa ndi zochitika zakuthupi ndi makhalidwe achirendo amasitha pamene zinthu za uzimu zatchulidwa.
5. Kusitha mu chikhalidwe ndi mayakhulidwe: Munthu yemwe amachita manyazi akhoza kusanduka kukhala wachiwawa. Zochitika komaso mawonekedwe amatha kukhuzidwaso. Makhalidwe abwino ndi nzeru zithaso kusitha. Mau amathaso kusitha. Onani Marko 5:9.
6. Kumatsana ndikuzuzika kwakukthupi: Mukhani yolowedwa ndi ziwanda, izi zimawonekera kwambiri pakuzungizika bongo. (Onani Mateyu 9:33; 12:22; Marko 5:4-5). Zikhozaso kuphatikizapo “kuzichekacheka” kapena kuwonongeka kwa thupi. (Onani Marko 9:14-29).
7. Kuzivulaza wekha kuthupi: pa Mateyu 17:14 pqli nkhani ya mwana wamamuna wa munthu wina amene amkaziponya yekha pamoto. Pa Luka 8:26-39 munthu ameneyu ogwidwa ndiziwandayu amkazicheka yekha ndi miyala kuzipweteka thupi lake.
8. Kuzuzika kwakukulu: Luka 8:28 imakamba kuti munthu ameneyu amkayenda mkumalira chifukwa chakuzuzika komwe kumkanchitikira mkati kobwera chifukwa chakugwidwa ndi ziwanda.
9. Kukanika kukhala bwino bwino: Munthu aneneyu amkalephera kukhala bwino bwino muzinda koma amkakhala kumanda. Onani Luka 8:27.
10. Kupyolera kunjira zoti siziri mmalemba: Kuthekera kolosera zakutsogolo kapena kuzindikira zomwe zirisosadziwika. Mkazi wapa Machitidwe 16:16 anali atalowedwa ndi mzimu wonenerera,

Zotsatirazi zikhoza kuwonetsaso kuponderezedwa, kugwidwa ndi kulamulirirdwa ndi ziwanda:

1. Kukhazikika muzonyasa monga ngati kutengpo mbali pakuchita makanema olaula, chigololo, dama, mathanyula, ndi machimo ena achiwerewere. Chilakolako champhamvu pakudya kosayenera, kuzimpha, kuzicheka ndi kupha ena.
2. Kukhala kapolo wa makhwala ozunguza bongo ndi mowa.
3. Masophenya ndi kulingalira komwe sikuchokera kwa Mulungu wowona.
4. Kumangidwa ndi nsinga monga ngati matha, nsanje, udani, miseche, kunyada ndizina zotero.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la Machiritso osawonera.

2. Kodi ndi ziwanda zitatu ziti zomwe zimachitira chiwembu thupi, moyo, mzimu wa munthu?

3. Kodi kufunika kwa mphatso yakuzindikira polimbana ndi mphamvu ya ziwanda mkotani?

4. Kodi zithanthauzanji kunena kuti kulowedwa ndi ziwanda?

5. Kodi ndimakhalidwe anji amene angawonetsedwe ndi munthu amene wagwidwa ndi ziwanda?

6. Zikutanthauza chati kunena kuti munthu akulamuliridwa ndi ziwanda?

7. Kodi ndi makhalidwe otani omwe amawonetsa munthu yemwe akulamuliridwa ndi ziwanda?

8. Zitanthauzani kulowedwa ndi ziwanda?

9. Ndimakhalidwe otani amene munthu walowedwa ndi ziwanda amawonetsa?

10. Fotokozani mmene satana amatengera ulamuliro.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwabukuli)

KUCHITA MAWU

Mwapephero ugundani nyengo yanu kapena ya wina amene inu mukumutumikira:

1. Kodi pali umboni wa mzimu wonyengerera umene ukugwira ntchito? Chifukwa chani mukuganiza choncho?”

3. Kodi pali umboni wa mzimu wobweretsa zowawa umene ukugwira ntchito? Chifukwa chani mukuganiza choncho?

4. Kodi pali umboni wa mzimu wonyasa umene ukugwira ntchito? Chifukwa chani mukuganiza choncho?

5. Nazo zizindikiro zoti munthu akuponderezedwa ndi ziwanda:

- Kumangidwa kwakuthupi.
- Kuponderezedwa kwammaganizo.
- Mavuto amaganizo.
- Mavuto amuuzimu.
- Zochitika.

Kodi pakuwoneka kuti pali kuponderezedwa ndi ziwanda? Chikukupangitsani kuti muganize choncho nchani?

6. Kugwiritsidwa ntchito ndi ziwanda kumazindikirika ndi:

- Kubwebweta kuzochitika zamatsenga
- Nthawi zonse kumangomuyamikira satana.
- Kumango khalira kuphunzira zinthu zasantana.

Kodi pakuwoneka kuti pali kugwiritsidwa ntchito ndi ziwanda? Chifukwa chani mukuganiza choncho?

7. Nazo zina mwa zizindikiro za kulowedwa ndi ziwanda:

- Kukhalamo kwa mzimu wonyasa.
- Kukhala ndi mphamvu zodabwitsa zakuthupi.
- Kutsutsa ku zinthu za uzimu.
- Kusitha kwa umunthu monga mau.
- Pamakhala kuzipweteka kuthupi.
- Samakhala bwino bwino
- Kuthekera kunena zakutsogolo zomwe zirizosadziwika munjira ya malemba.
- Kuzipweteka thupi.

Kodi pakuwoneka kuti pali kugwidwa ndi ziwanda? Chifukwa chani muganiza choncho?

8. Kumbukirani: Zotsatirazi zimawonetsaso kulowedwa, kuponderezedwa, ndikugwiritsidwa ntchito ndi ziwanda.

- Kugwidwa ndi makhalidwe oipa achiwerewere monga kutengapo mbali pojambula kanena olawula, chiwerewere, zadama, kugonana amuna kapena akazi okhaokha komaso ndi machimo ena okhudzana kugonana. Chilakolako cholimba pakudya mosayenera, kuzipha, kupha.
- Kukhala kapolo wa makhwala ozunguza bongo, ndi mowa.
- Kuwombeza, masomphenya, kulingalira zomwe sizika chidwi kapena sizivhokera kwa Mulungu mmodzi wowowna.
- Kumagwidwa kwa maganizo monga matha, khawa, kukhumudwa, udani, nsanje, kukamba miseche, kunyada, kumangolingalira zoipa.

CHAPUTALA 18

KUTUMIKIRA MAMASULIDWE

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziroli mukuyenera kukaniritsa zinthu izi:

- Kulumba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kuwonetsera yemwe akuyenera kuthana ndi mphamvu ya ziwanda.
- Kufotokoza zokozekera zoyamba poitumikira mamasuridwe.
- Kulemba mwachidule ndondondomeko zotumikirira mamasuridwe.

LONJEZANO LA MACHIRITSO:

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

CHIYAMBI

Pali anthu ochuluka amene amangidwa ndi satana munthenda zimene zimayamba ndi ziwanda. Palinso ena ochuluka amene akuzuzika poponderezedwa, kulowedwa, ndi kugwiritsidwa ntchito m'dzanja la mdani. Muphunziro lino muphunzira kuti ndindani amene akuyenera kuthana ndi mphamvu zaziwanda, makozekeredwe a utumiki wamamasuridwe, ndi mmene mamasuridwe agatumikidwire.

KODI NDINDANI AMENE ANGALIMBANE NDI MPHAMVU YA ZIWANDA?

Kuthana ndi mphamvu ya ziwanda sichinthu choti chingosiridwa kwa atumiki owerengeka. Yesu anati okhulupirira onse ali ndikuthekera kogonjetsa mphamvu ya ziwanda.

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano. (Marko 16:17)

Yesu anapereka kwa ophunzira Ake kuthekera kulimbana ndi mphamvu ya ziwanda. Koyambirira anapereka mphamvu zimenezo kwa atumwi:

Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa. (Marko 6:7)

Anaperekaso mphamvu yomweyo kwa okhulupirira onse:

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; m'dzina langa adzaturutsa ziwanda... (Marko 16:17)

**Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda:
munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)**

palibe umboni wina uliwonse Mmalemba okhulupirira Mulungu kuti utumiki ofunikawu kuti ndi wawa anthu ochepa chabe. Mwachitsanzzo, munthu wamba Filipino anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kutulutsa mizimu yoipa ku Samaliya (Machitidwe 8).

Iziz sizikutathauza kuti okhulupirira akuyenera kuthamanga mwasanga kukalimbana ndi mphamvu ya ziwanda popanda kukozekeka bwino, monga mmene anachitira ana A Skeva (Machitidwe 19). Ndikofunikaso kuti okhulupirira asamangokhalira kulingalira zaziwanda. Sitinayitanidwe kuti tikhale akatswiri aziwanda. Palibe mphamtso ya uzimu “yotulutsira ziwanda.” Koma simukuyera kuwopa mphamvu ya ziwanda. Pamene mwakumana ndi onse amene akhudzidwa ndi ziwanda, mukuyenera kukhala ndi mphamvu yobweretsa mamasuridwe ochokera kwa Mulungu.

KUTUMIKIRA MAMASULIDWE

Nazo zina mwandondomeko potumikira mamasuridwe kwa anthu omwe akhudzidwa ndi mphamvu ya ziwanda.

KUZIKOZEKERETSA INU MWINI:

Chikhulupiriro chimadza pakumva Mawu a Mulungu, makamaka “Rhema” (Mawu oyankhulidwa ndi Mulungu). Yambani kumanga chikhulupiriro pantima panu powerenga Chipangano Chatsopano pokhala ndi malingalironso atsopano:

- Chilichonse chimene Yesu anawauza omutsatira Ake kuti achite, mukuyenera kuyamba kuchita.
- Chilichonse chimene anati Achita, dikirani kuti Azazicitadi.
- Ngati anati mukhoza kumasula onse amene akuzuzidwa ndi satna, nde yembekezani kuwona iwo akumasulidwa.
- Ngati anati kutulutsa ziwanda, nde chitani choncho mu dzina Lake ndipo yembekezani kuti iwo akumverani.

Kanani ziphunzitsa zonse za munthu ndi kusindikira kwanu komwe mulinako. Vomerani kuti Chipangano Chatsopano chimatanthauza zeni zeni zomwe chimanena. Zindikirani kuti ndi chowonadi ndipo chitani moyenera. Ndinu kazembe wa Khristu (2 Akorinto 5:20) kazembe samakayika kuti dziko lomwe lamtumiza kuti akaliyimirire likhala kumbuyo kwa mau ake.

Salani kudya ndi kupemphera musanayambe kutumikira mamasulidwe. Popeza mphamvu ndi ulamuliro zakumasula zimachokera kwa Mulungu, nde mkoyenera kuti pakhale kulumikizana! Ziwanda zina zimatuluka ndi ndi pemphero ndi kusala kudya. Yesaya 53 imaphunzitsa kuti Mulungu amalemekeza kusala kudya komwe kumaika chikwa pazosowa za ena.

KUWAKOZEKERETSA ENA:

Ngati kuli kotheka, gulu la okhulupirira likuyenera kugwiritsidwa ntchito pomanga komaso kutulutsa ziwanda. Yesu anatumiza ophunzira Ake awiriawiri ku utumiki umenewu:

Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza Iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa. (Marko 6:7)

Izi sizikutathauza kuti simungatumikire nokha kwa munthu amene wagwidwa ndi ziwanda pamene mwakumkana naye, koma muli mphamvu mugwirizano wa pemphero ndi okhulupirira ena. Popeza mpohamvu zimachokera mugwirizano, nde onse amene akuyanjanana nanu mu utumiki wa mamasuridwe akuyenera kukhala okozekera mupemphero ndi kusala kudya.

Ngati muzakumane ndi munthu amene wagwidwa ndi ziwanda kuti apemphereredwe koma opanda malangizo abwino, ziringati kumukakamiza osakhulupirira kuti amvomere Yesu kuti ndi mpulumutsi wake popanda kuzindikira kuti Iye ndi ndani, zindikirani tchimo ndi kufuna kwawo kwachipulumutso. Pamene mukugawa Uthenga Wabwino wanzeru ofuna kupindula moyo samakakamiza kuti apange chisakho mwachanguchangu. Pali utumiki woyambirira umene ukuyenera kuti uchitiki. Malangizo abwino akuyenera kuperekedwa.

Izinso ziri chimodzimidzi ndi mamasuridwe. Nthawi zina, Mulungu amamasula popanda malangizo oterewa. Koma potumikira mamasuridwe mukuyenera kugwiritsa ntchito njira ina iriyonse imene inaperekedwa ndi Mau a Mulungu kuti muwone kuti ntchito yagwirika. Chikhulupiriro ndi njira imodzi imene mphamvu ya Mulungu yomasula ndipo imabwera pakumva Mau a Mulungu, nde malangizo ndiofunika kwambiri. Yesu anasakaniza kulalikira ndi kuphunzitsa pamodzi ndi kuchiritsa komaso kumasula ndipo analangiza omutsatira Ake kuti akachitenso chimodzimidzi.

MALO OCHITIRAPO UTUMIKI:

Kutumikira mamasuridwe kwa onse amene akhudzidwa ndi mphamvu ya ziwanda kukhoza kuchitika pa nthawi yomwe mapemphero alimkati mkachisi. Utumiki umenewu sukuyenera kungokhala pamalo obisika basi. Ndi utumiki umene uli wamoyo mu mpingo.

Yesu anatumikira kwa ogwidwa ndi ziwanda monga ngati mbali imodzi ya selevisi ya mpingo (Marko 1:21-25). Komabe, sikofunika kuchita kudikira kuti mpingo ukumane kaye kuti munthane ndi mphamvu ya ziwanda. Yesu anabweretsa mamasulidwe paliponse ndi nthawi iriyonse imene wakumana ndi ziwanda.

NTHAWI YOTUMIKIRA:

Pamene mwakonzeka kuti mutumikire machiritso...

1. Yambani kulambira ndi kutamanda:

Timalowa mukupezeka kwake (pamene pali mamasulidwe ndi machiritso) kupyolera pakulambira ndi kutamanda. Mamasuridwe akhoza kubwera kupyolera pakulambira ndi

kutamaba, ngakhale patakhalala kuti palibe kutumikira ndi mapemphero chifukwa Mulungu amapezeka mmalambiro a anthu Ake. Pamene tikutamanda, Amapezeka kuti achiritse ndi kumasula.

2. Kukonza malo achikhulupiriro:

Munayamba kale kuchita izi pamene matumikira Mau a mamasuridwe, koma mukuyenera kutengaso sitepe yowonjezera pokoza malo kukhala achikhulupiriro. Kusakhulupirira kumatchinga ngakhale utimiki wa Yesu ku Nazarete. Nthawi zina Yesu amkathamangitsa osakhulupirira akamatumikira (Marko 5:35-40). Nthawi zina amatha kuwatsogolera anthu kutuluka mmidzi mwawo (munyengo yosakhulupirira) ndicholinga choti awatumikire (Marko 8:23). Mwananyengo zina monga momwe Mulungu atatsogolerere, mukuyenera kuwafusa onse omwe akuvutika ndi kusakhulupirira, matha, ndizina zotero... kuti asiye.

3. Yambani ndikupemphera:

Funsani nzeru ndi chidziwitso musanayambe kutumikira mamasuridwe. Nthawi yamapemphero, Mulungu antha kuwonetsera kwa inu...

- Mau achidziwitso: Mfundo zapaderadera ndi mbiri ya munthu kukhudzana ndi mmene aliri potero ndemuzadziwa kapemphereredwe kake. “Mau a chidziwitso” kukhoza kuphatikizapo kuzindikira mwakuya mu uzimu mwanu, maganizo, mau, kapena pazويمvaimva. Mau achidziwitso akhoza kubvumbulutsa kuti matendawo ndiotani kapena chifukwa chimene munthuyo ali munyengo imeneyo.
- Vesi yammalemba: Mau a Rhema anyengo imeneyo, munthu kapena gulu.
- Masomphenya: zinthuzi mmaso ammalimgaliro okhudzana ndi yemwe mukumtumikirayo.
- Mau achikhulupiriro: Mau apaderadera achilimbikitso ndi chikhulupiriro chifukwa chamunthuyo.
- Kudzodza kwapaderadera: Kudzadzidwa ndimphamvu mwadzidzi, kumakhala pa mtima, kapena mpamvu zopereka kulimbika mwapaderadera.

4. Funsani mafunso ochepa:

Izi ndizosafunika. Ndichisakho ndipo zikuyenera kuchitika malingana ndi mmene Mulungu angatsogolere. Mulungu atha kukupatsani mau anzeru mwapaderadera okhudzana ndi nyengo yamunthu ndipo simukuyenera kumufunsaso mafunso.

Koma ngati Mulungu sabvumbulutsa chinachironse kwa inu, musakayike kugwiritsa ntchito njira yofunso mafunso. Yesu anagwiritsa njira zonse yakuthupi ndi yakuuzimu. Pa nthawi zina amkatha kuzindikira nyengo ya anthu ndi Mzimu Woyera. Nthawi zina amkawafunsa mafunso pachomwe akufuna ndi nthawi imene akhalira akuzuzika.

Kufusa mafunso kumakuthandizani kuti mupeze mbiri kuti mukathe kupemphera mwachindunji. Kumakuthandizano kuzindikira ngati munthuyo akufunika malangizo ena musanayambe kupemphera. Yesu amkakonda kuchita zimenezi. Amkawafunsa anthu mafunso okhudzana ndi chikhulupiriro chawo ndipo kenako amathana ndi mphamvu zakusakhulupirira asanawatumikire. Onani zitsanzo zotsatirazi:

- Marko 5:1-20 Yesu anafusa mafunso munthu waziwanda.
- Marko 8:22-29 Munthu wosawona anafusidwa mafunso.
- Marko 9:14-27 Nyamata wamzimu woyipa.
- Marko 10:46-52 Batumeyo afusidwa mafunso.

Muzimufunsa munthu kuti mvuto ndi chani? Kuyakhula mopempha mwapemphero mkofunika. Yesu anamasula anthu ambiri omwe anadza kwa Iye omwe anamuza zofuna zawo. Kupempha pakokha kulingati kuchita mwachikhulupiriro chomwe chimabweretsa chiyambi chamachiritso (Yakobo 5:14-15). Mukungofuna choonadi chochepa. Simufunika kuti mudziwe mbiri yonse yamoyo yawo.

Mufunsi munthu amene atapempheredweyo kuti, “Kodi kukhulupirira kuti Yesu akhoza kukumasula?” Ngati amvomera, nde afunsi kuti, “Mukhulupirira kuti Yesu antha kuchizi izi pompano?” Ngati yankho lawo ndi “ayi” kumafunso onsewa, pamenepa ndekuti pakufunika malangizo oonjezera ochokera m’Mau a Mulungu.

5. Zinfikirani mvuto leni leniro:

Gwiritsani ntchito uthenga omwe mwapeza pa nthawi imene mafunsa mafunso kapena nzeru zimene Mulungu wakupatsani kuti muzindikire ngati mvutolo liri la:

Lakuuzimu: Mavuto okhudzana ndi tchimo. Awa amafunika utumiki wa machiritso auzimu (Chipulumutso, kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo).

Zakuthupi: Matenda akuthupi amene amayamba ndi kuzuzidwa ndi mizimu yaziwanda.

Maganizo: Mavuto okhudzana ndi kudera khawa, matha, mkwiyo, kaduka, kukaika, kulephera, nsanje, kuzikonda, kusokonezeka, kukhumudwa, kusakhululuka, zochitika zakale.

Izi zimatchulidwa kuti “machiritso amkati,” koma liwuli lagwiritsidwa ntchito udyo. Sikofunika kubwereranso mbuyo pochita zokozekerra paza mfundo ndi maganizo. Sikoyenera kukhala ndi masabata, miyezi, kapena zaka kuti muchiritsidwe kumavuto amenewa. Ngati mungachite zimenezi ndekuti mukuyesera kuchiza munthu wakale mmalo mowathandiza iwe kuti akhale cholengedwa chatsopano mwa Khristu.

Tinayitanidwa kukhala atumiki oyanjanitsa (2 Akorinto 5:18-21). Kuyanjanitsidwa kukuphatikiza kwa Mulungu ndi munthu, ndipo apa mpamene machiritso amkati amabwerera.

Mukuyenera kumuphunzitsa munthu yemwe akufuna kukhululukira. Sikuti ndi:

- Kulungamitsa zolakwa zawina zomwe akuchitirani. (Mwachitsanzo, kunena kuti, ” pochita zimenezi anali atapanikizika.”)
- Sikukana kuti pachiyambi munamvulazidwa.
- Kukana zomwe zinachitidwa kwa inu.
- Kudikira nthawi yochiritsidwa pakumvulazidwa. (Sichoncho).

Kukhululuka kweni kweni kumabwera ndi:

- Kumvomereza kuti zomwe zinachitika kwa inu zinali zolakwika, ndizochita za anthu ochimwa mudziko la uchimo. Sikufunika kubwereraso pambuyo kumakakumbukiranso zomwe zinachitikazo, koma mmalo mwake mukhoza kuthana nazo pozikana. Mvomerezani zomwe zinachitikazi ndi momwe zinakhudzirani.
- Perekani kumvulazidwa kwanu kwa Mulungu ndipo Mumupemphe kuti akuchiritseni kumaganizo oipa. Simungaiwaliretu choonadi cheni cheni cha zomwe zinachitika ndi mmene zinakuhudzilani koma chomwe mukufunika ndi machiritso pa zoipa pa zomwe zinakuchitikirani.
- Kumphepha Mulungu kuti akuthandizeni kukhululukira ena omwe anatengapo mbali, nde akhululukireni iwo monga momwe Kristu amakukhululukirani inu. Zindikirani kuti Mulungu akukhululukirani pamene inu mukukhululukiranso ena: “Mutikhululukire ife zolakwa zanthu monga ifenso tikhululukira amangawa anthu.” Munthu akuyeneranso kuzikhululukira yekha (kumva kulakwa pazolakwa zimene wachita) ndipo akuyenera kupempherera machiritso pa maganizo ake. Nazo ndondomeko za momwe munthu angazikhululukire yekha:
 - Mvomerezani tchimo lomwe likukupangitsani kulakwa ndi maganizo auchimo, mvomerezani kwa Mulungu, ndipo lapani. Mpempheni kuti akukhululukireni machimo anu ndipo achiritse maganizo anu.
 - Zindikirani kuti Mulungu akakhululuka, amaiwala (amawaponya kutali machimo anthu monga mmene kuliriri kutalikana kwa kummawa ndi kumadzulo).

- Nenani 1 Yohane 1:8-9.

Zamuubongo: Mavuto ochokera pakuyamba moganiza molakwika, chiwembu cha satana maganizo, kusaganiza bwino. **Kumbukirani:** chifukwa munthu ndi utatu, nde mavuto ambali imodzi amakhudza munthu yense. Pamene mukutumikira, nthanani ndi munthu yense, osati mbali imodzi yokha. Munthu ndi thupi, moyo ndi mzimu. Uthuthu ukutanthauza kuti kuthana ndi zonsezi.

6. Zindikirani ngati iri nthawi yoyenera kupemphera:

Zindikirani ngati iri nthawi yoyenera kapena ayi kupemphera pemphero lamachiritso. Nthawi zina, muzapemphera, koma nthawi zina, musazadabwitsidwe pamene Ambuye azakutsogolereni kuti musapephere kapena muchedwerepo.

Yesu anachedwetsapo machiritso a mwana wa mzimayi waku Sifulina ndi Lazaro. Sanachite ntchito zambiri ku Nazarete chifukwa chakusakhulupirira kwawo. Mulungu atha kukutsogolerani kuti muchedwerepo kufikira atazakupatsaniso malangizo ena, monga ngati akuyenera kuthana kaye ndi mvuto la tchimo, kapena kufuna malangizo ena pamamasulidwe.

7. Pempherani pemphero la mamasulidwe:

Pempherani pemphero la mamasulidwe lomwe limapita chindunji kumvuto la ziwanda lomwe mwalizindikira. Simukuyenera kumukakamiza Mulungu kuti amasule chifukwa cha pemphero lanu. Monga momwe chipulumutso kuti chilipo kale, zirinso chimodzimodzi ndi mamasulidwe. Monga mmene chiriri chipulumutso kuti chimabwera ndi chikhulupiriro, nde nchimodzimodzisozomamasulidwe. Mulungu akufuna kumasula, mangaso mmene amafunira Atapulumsa. Ngakhale kuti mphamvu ya Mulungu nthawi zina imapezeka munjira yapaderadera yomasula (Luka 5:17). Mukhozabe kupitiriza kupemphera popanda kudzodza kwapaderadera kuchita choncho chifukwa Yesu anakulamulani kuti mutero monga mmene Iye anakuzirani kuti mufalitse Uthenga Wabwino.

Gwiritsani ntchito anthu ena kuti akuthandizeni kutumikira ngati muli pa gulu. Pamakhala kuchulukitsa kwa mphamvu ya uzimu pamene anthu ambiri akupemphera pamodzi (Mateyu 18:19).

Yesu ananena kuti koyamba mukuyenera kumanga kaye mdani, kenako nde munthu kumugonjetsa:

Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lace. (Mateyu 12:29)

Ngati mphamvu ya ziwanda yopendereza ndiyochechera kunja, pempherani kuti goli lake liduke ndikutiso kuti mphamvu yawo imangidwe. Mwachitsanzo, Yesu anamasula mzimayi mu Sunagoge ku mzimu wakumva zowawa. Sikuti analowedwa ndi ziwanda, koma anaponderezedwa. Kutulutsa sikunali koyenera.

Ngati nkhani yake iri yolowedwa ndi ziwanda, muli ndi ulamuliro otulutsa ziwanda mudzina la Yesu. Siulamuliro mumphamvu zanu kapena kuthekera kwanu, koma mudzina Lake. Ndikofunika kwambiri kugwiritsa ntchito dzina la Yesu panthawi yakutulusa ziwanda.

Chikhulupiriro, kusala kudya, ndi kupemphera ndizofunika potulutsa ziwanda. (Werengani zomwe zinachitika pa Mateyu 17:4-21). Izi nchifukwa chake kukozekeka musanayambe kutumikira mkoyenera. Mau a Mulungu (Aefeso 5:17; Ahebri 4:17); mwazi wa Yesu (Chibvumbulutso 12:11), ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Machitidwe 1:8; 2:38) ndizidaso za mamasulidwe zomwe Mulungu wapereka.

Kuukira kapena kulalatira ziwanda sikofunikira. Ndi udindo wanu mu dzina la Yesu lomwe limachititsa kuti izo zituluke, osati kufula kwa mau anu panthawi ya mapemphero amamasulidwe. Nthawi zonse kanizani kuti ziwanda zikuloweniso. Iri ndi gawo lofunika kwambiri papemphero la mamasulidwe:

Ndipo pamene Yesu anaona kuti khamu la anthu lirikuthamangira pamodzi, anadzudzula mzimu woipawo, nanena ndi uwo, Mzimu wosalankhula ndi wogontha iwe, Ine ndikulamula iwe, turuka mwa iye, ndipo usalowenso mwa iye. (Marko 9:25)

Musayerekeze kutumiza ziwanda ku Gahena. Yesu ndi ophunzira Ake sanachite zimenezi. Tiri ndi ulamuliro okha omanga, omasula, ndikutulutsa. Pali nthawi yoyikika yachiweruzo chomaliza cha ziwanda mtsogolo. Ziwanda zinati kwa Yesu:

...Tilinanu chanu, Yesu, Inu Mwana wa Mulungu? Kodi mwabwera kuzatizua ife NTHAWI ISAKWANE? (Mateyu 8:29)

Pemphero la onse amene akhudzidwa ndi ziwanda likhoza kuchitika popanda kusanjika manja. Yesu anagwiritsa ntchito kusanjika manja potumikira kwa mzimayi oponderezedwa ndi mizimu yozuza pa Luka 13:11-13. Mmalu mwina, Sanasanjike manja koma mmalo mwake anangoyakhula kwa ziwanda (Luka 9:42).

8. Mulemekzeni Mulungu chifukwa cha yankho:

Pemphero litsatane ndi kupereka malemekezo kwa Mulungu chifukwa chamamasulidwe. Kumbukirani pachitsanzo cha m'Baibulo pa anthu khumi akhate omwe anachiritsidwa, onse anachiritsidwa koma mmodzi yekha anabwerera kukamuyamika chifukwa chakuchiritsidwako. Kuyamika mwa chikhulupiriro osati mowoneka. Mwachita zimene Mau a Mulungu amanena kuti tichite. Khulupirirani kuti wachita zomwe analonjeza kuti azachita. Muyamikeneni Iye chifukwa cha izi.

ZINDIKIRANI ZIZINDIKIRO ZAMAMASULIDWE:

Pankhani yolowedwa ndi ziwanda, nthawi zina ziwanda zimatuluka mwamavuvu, monga ngati kulira, kapenaso kumugwetsa munthu pansu. Pamene ziwanda zachoka (Kaya mkulowedwa kapena kuponderezedwa), pamakhala kumva kwakumasuridwa, chimwemwe, monga ngati kuchotsedwa kwa chithu cholemera.

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la MACHIRITSO osawonera.

2. Malingana ndi Malemba, kodi ndindani amene akuyenera kuthana ndi mphamvu ya ziwanda?

3. Lembani mwachidule ndondomeko zozikozekeretsa nokha potumikira mamasuridwe.

4. Lembani mwachidule ndondomeko zazokozekera potumikira mamasuridwe kwa ena.

5. Lembani mwachidule ndondomeko zimene zakambidwa mu phunziro lino zotumikirira mamasuridwe.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

1. Onani zolembedwa ndi Baibulo za utumiki wa Yesu kwa onse amene anali ndi mvuto amene anabwera ndi machitachita aziwanda:

- Mkazi wolumala: Luka 13:10-17
- Munthu wa mzimu woyipa Msunagoge: Marko 1:23-28; Luka 4:31-37
- Munthu wa ziwanda waku Galireya: Mateyu 8:28-32; Marko 1:23-28; Luka 4:31-37
- Mkazi wa nthenda yamwazi: Mateyu 9:20-23; Marko 5:25-34; Luka 8:43-48
- Mkazi wa Kukanani: Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30
- Mwana wamizimu yoyipa: Mateyu 17:14-21; Marko 9:14-29; Luka 9:37-49
- Ziwanda zoletsa kuyakhula: Mateyu 17

Zochitika zina: powonjezera pozochitika zapaderadera zomwe Yesu anachita, Baibulo limakamba zina za utimiki Wake kwa amene anakhudzidwa ndi mphamvu ya ziwanda:

- Muzolembedwa zotsatirazi mau oti “Kuchiritsidwa” agwiritsidwa ntchito kuwonetsera mmene Yesu anathanirana ndi ziwanda: Mateyu 4:24; Luka 6:18
- Muzolembedwa zotsatirazi mau oti “kutulutsa” agwiritsidwa ntchito kuwonetsa ndondomeko Yake: Marko 1:32-34,39; 6:13
- Luka 4:41 inangolembea kuti ziwanda “zinatuluka.” Luka 7:21 imati “anachiritsa” iwo. Mateyu 8:16 imati Iye “anazitulutsa izo ndi Mau Ake.” Marko 16:9 ndi Luka 8:2-3 inanena kuti Yesu anatulutsa ziwanda zisanu ndi ziwiri mwa Mariya waku Magadala. Muchigulu, Yesu sanalole kuti ziwanda ziyakhule: Marko 1:

2. Muphunziro lomaliza muzazindikira ngati nyengo yanu kapena yawina amene mukumutumikira inabwera ndi ziwanda. Kutengera zimene mwaphunzira mu chaputala chino, mungapitirire bwanji kutumikira mamasuridwe?

3. Ndondomeko zotsatirazi zatengedwa kuchokera muphunziro lino kuti inu mugwiritse ntchito potumikira mamasuridwe:

ZOKONZEKERA ZOYAMBA

Mwanokha:

___ Werengani Mau a Mulungu okhudzana mamasuridwe.

___ Salani kudya ndi kupemphera.

Kwa ena:

Munyengo zina zomwe munthu wakhudzidwa ndi ziwanda munthu amaloleza, ndondomeko zotsatirazi:

- ___ Malangizo oyenera okhudzana mamasuridwe.
- ___ Werengani Mau a Mulungu okhudzina ndi mamasuridwe.
- ___ Kusala kudya ndi kupemphera mamasuridwe asanayambe.

NTHAWI YOTUMIKIRA:

- ___ Pangani kuti malo akhale achikhulupiriro.
- ___ Pempherani chidziwitso. Mulungu antha kukupatsani:
 - Mau achidziwitso
 - Vesi lochokera Mmalemba
 - Masomphenya
 - Mau achikhulupiriro
 - Kudzodza kwapaderadera
 - Kuchita kwapaderadera kwa chikhulupiriro
- ___ Funsani mafuso ochepa.
- ___ Muzindikire kuti mvuto ndi chani
 - Zochoka ku uzimu
 - Zochoka kuthupi
 - Zochoka kumaganizo
 - Zochoka mmaganizo
- ___ Zindikirani ngati iri nthawi yopemphera kapena ayi.
- ___ Pempherani pemphero lamamasuridwe
- ___ Mulemekezeni Mulungu chifukwa chayankho
- ___ Zindikirana zizizndikiro zamamasuridwe

CHAPUTALA 19

UTUMIKI WAMAMASULIDWE WOLONDOLA

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziroli mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kulemba mwachidule ndiondomeko za chisamaliro cholondola kwa onse amene alandira mamasuridwe.
- Kulemba mwachidule ndondomeko zoteteza ku mphamvu ya ziwanda.

LONJEZANO LA MACHIRITSO:

Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)

CHIYAMBI

Yesu ananena mosabisa kuti chisamaliro chowalondola onse amene amasulidwa ku machichita aziwanda ndi chofunika kwambiri, Iye anati:

Koma mzimu wonyansa, utaturuka mwa munthu, umapitirira malo opanda madzi kufunafuna mpumulo, osaupeza.

Pomwepo unena, ndidzabwerera kunka kunyumba kwanga, konkuja ndinaturukako; ndipo pakufikako uipeza yopanda wokhalamo, yosedwa ndi yokonzedwa.

Pomwepo upita, nutenga pamodzi ndi uwu mizimu yina inzace isanu ndi iwiri yoipa yoposa mwini yekhayo, ndipo ilowa, nikhalamo. Ndipo 4 matsirizidwe ace a munthu uyo akhala oipa oposa mayambidwe ace. Kotero kudzakhalanso kwa obadwa oipa amakono. (Mateyu 12:43-45)

Pamene mzimu wonyasa watulutsidwa, pamakhala zotsatira zauzimu kuti pamalopo pamakhala popanda kanthu. Ngati dzenje limeru sirikwiridwa ndi kupereka chisamaliro cholondola, mphamvu zaziwanda ziambwereraso mwamphamvu kwambiri.

CHISAMALIRO CHOLONDOLA

Izi ndi ndondomeko zofukwa pa chisamaliro cholondora kwa onse amene alandira mamasuridwe:

1. PEMPHERANI PEMPHERO LOKANA:

Potsatira kumasuridwa, ku onse amene analowedwa ndi ziwanda akuyenera kutsogoleredwa kupemphero lovomereza, lolapa, ndi lokana tchimo la mtundu wina uliwonse kapena chinachirichose chimene chalumikizana ndi machitachita aziwanda.

2. ONONGANI ZITNHU ZAZIWANDA:

Ngati munthu ali ndizinthu zaziwanda (mafano, zinthu zaufiti, mabuku, ndi zina zotero.), izi zikuyenera kuonongedwa.

3. DZADZANI MALO AUZIMU OPANDA KANTHU:

Pamene chiwanda chatuluka, chimafunafuna thupi lina limene chizigwiritsa ntchito. Chiwanda chimakhala chosowa ntendere chikakhala kunja kwa thupi la munthu. Ndikupyolera kukhala mwamunthu ndi kutenga ulamuliro wa moyo wake ndipamene satana amatha kukwaniritsa zolinga zake zoipa.

Chifukwa pali kuopsya kuti ziwanda zinthu kubwereraso kwa munthu wakale ndipo zimabwerano ndi mizimu yanyasitsitsa, dzenje la uzimu likuyena kukwiriridwa. Munthu akuyenera kulandira Yesu Kristu monga ngati Mpulumutsi ndikudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Akuyenera kupitiriza kuzimiza yekha mupemphero ndi Mau a Mulungu ndipo mwasangasanga akhale mbali imodzi ya okhulupirira.

4. PEREKERANI UMBONI WANU:

Onse amene amasuridwa ku mphamvu ya ziwanda akuyenera kuchitira umboni okhudzina ndi mamasuridwe awo. Yesu anamuza munthu womasuridwa kuziwanda wa ku Gerasa:

Ndipo sanamlola, koma ananena naye, Muka kwanu kwa abale ako, nuwauze zinthu zazikuru anakucitira Ambuye, ndi kuti anakucitira cifundo. Ndipo anamuka nayamba kulalikira ku Dekapoli zinthu zazikuru Yesu adamcitira iye; ndipo anthu onse anazizwa. (Marko 5:19-20)

Chibvumbulutso 12:11 imatsimikiza kuti timalaka mphamvu za satana ndi mau aumboni wanthu.

5. ZITETEZENI NOKHA KUMPHAMVU YA ZIWANDA:

Izi ndi njira zapaderadera zomwe zingakuthandizeni kuti muziteteteze nokha kumachitachita amphamvu ya ziwanda:

-Chitetezo chofunika kwambiri ndi kulandira Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi wanu chifukwa ziwanda sizingamulowe munthu wobadwa mwatsopano. Kutsatira

kupulumutsidwa kwanu kumachimo, popeza pakupyolera ku ntchimo “mapereka mpata kwa satana” kapena mapereka mwayi kwa iye kuti azikuzuzani.

-Dzadzidwani ndi Mzimu Woyera. Mizimu ya ziwanda ndi Mzimu wa Mulungu sangakhale mwa munthu mmodzi.

-Pewani kuika chidwi paziwanda. Sikulakwa kuphunzira zimene Mau a Mulungu amanena zokhudzana izo kapena phunziro limene lakhazikika pa Mau a Mulungu, koma musamawerenge mabuku achikunja, kupita kowombeza, ndizina zotero, kuphunzira zambiri zaziwanda.

-Pewani kulumikizana kulikonse ndi ziwanda. Musamapite kwa asing’anga, owombeza, ndi ena otero. Musamatumikire milungu yonama kapena kulola mafano kuti akhale mnyumba mwanu (Deutoronome 7:25-26).

MAYESO OZIYENSA NOKHA

1. Lembani lonjezano la MACHIRITSO osawonera.

2. Lembani mwachidule ndondomeko za chisamaliro cholondola kwa onse amene alandira mamasuridwe.

3. Lembani mwachidule ndondomeko pachitetezo kumphamvu ya ziwanda.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

KUCHITA MAWU

Ngati inu kapena wina wake amene munamutumikira walandira mamasuridwe, lembani mmene inu mungachitire...

Kupemphera pemphero lokana:

Kuwononga zinthu zaziwanda:

Kudzadza malo auzimu ongokhala:

Kuperekera umboni wanu:

Zitetezeni nokha kumphamvu ya ziwanda:

GAWO LACHISANU NDI CHIWIRI

CHIKHALIDWE CHA UFUMU WA MULUNGU

Kumayambiriro a phunziro lino munaphunzira za nkondo yayikulu pakati pa ufumu wa satana ndi Ufumu wa Mulungu imene imaziwonetsera ku uzimu wa moyo ndi uzimu, ndi kuthupi.

Mwaphunzira zikhudzna ndi chiwembu cha mdani pa thupi kupyolera kukudwala ndi kulimbana ndi machiritso akumwamamba amene anaperekedwa kupyolera pa imfa ya Yesu Kristu.

Mwaphunziraso ndondomeko zotumikirira ndi kulandira machiritso ndi mamasuridwe.

Mugawo lino lomaliza, muphunzira mmen mungakhalire mu Ufumu wa Mulungu monga ngati womenya nkondo.

CHAPUTALA 20

OMENYA NKHONDO ABWINO

ZOLINGA:

Pamapeto pa phunziro lino mukuyenera kukwaniritsa zinthu izi:

- Kulemba lonjezano la MACHIRITSO osawonera.
- Kulemba mwachidule ndondomeko za Baibulo zoyendera munthanzi lakumwamba.
- Yendani mu nthanzi la kumwamba monga ngati wankhondo wabwino.

LONJEZANO LA MACHIRITSO:

Udzikondweretsenso mwa Yehova; Ndipo iye adzakupatsa zokhumba mtima wako. Perekani njira yako kwa Yehova; Khulupiriranso Iye, adzacicita. (Masalmo 37:4-5)

CHIYAMBI

Ndikovuta kumenya nkhondo yauzimu kulimbana ndi satana ndi asirikali ake oipa pamen muliofoka, odwala, ndimuululu waku thupi. Ichi nhifukwa chake satana anabweretsa ziwembu zolimbana nanu. Amadziwa kuti simungakhale msirikali wamphamvu monga sirikali wa uzimu pamene inu mukudwala.

Mwaphunzira ndondomeko zotumikirira ndi kulandira machiritso, koma Baibulo lirindizambiri zoti linene zokhudzana ndi mmene mungatetezere thupi lanu ku ziwembu za satana. Baibulo limaphunzitsa ndondomeko zokhalira mu Ufumu wa Mulungu kuthupi ngakhaleso ku uzimu.

Zotsatirazi ndi chitsogozo cha ndondomeko zolandira ndikukhala mu moyo wa nthanzi. Zonse zimathandiza kupewa kapena kuchiritsa. Ndikofunika kuti mudziwe ndondomeko zimenezi kuti potero muntha kugawanaso ndi ena ndikuti pakuchita mwanzeru mukathe kuyanjana ndi Mulungu muzitnthu zokhudza nthanzi la thupi ndi mamachiritso. Mulungu amafuna omenya nkhondo abwino.

LANDIRANDIRANI YESU KUKHALA MPULUMUTSI:

Pamene mwachita chonchi, makhala Khristu wobadwaso mwatsopano, mwana wa Mulungu. Baibulo limaphunzitsa kupyolera munkhani ya mkazi wa Suro-Fonika kuti machiritso ndi “mkate wa ana,” kuti ndiwa ana a Mulungu (Marko 7:24:30).

Chisomo cha Mulungu chimachiza anthu osakhulupirira ndipo amagwiritsa ntchito kumabweretsa iwo ku chipulumutso, koma machiritso alidi mkate wa “ana a Mulungu”. Polandira Yesu kukhala Mpulumutsi, mazika nokha pamalo poti mukhoza kulandira machiritso akuthupi.

Ngati ndinu okhulupirira kale ndipo mwachimwa, gwiritsani ntchito cholowa chanu chopempha ndikulandira chikhululukiro (1 Yohane 1:8-9). Pozisunga nokha popitiriza poziyeretsa, mapewa matenda amene amabwera chifukwa chamachimo anu.

MPATSENI MULUNGU KACHISI WAKE:

Thupi lanu ndi kachisi wa Mulungu. Perekena thupi lanu kwa Mulungu pazolinga Zake: 1 Akorinto 6:13, 19-20; Aroma 12:1.

MUNTHANGE MWAFUNA UFUMU WA MULUNGU:

Pamene mwathanga mwafuna Ufumu wa Mulungu, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezereka kwa inu (kumphatikizapo nthazi): Mateyu 6:33

MUDZADZIDWE NDI MZIMU WOYERA:

Yesu sanachiritse kufikira Atadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Baibulo limaphunzitsa kuti mpingo woyamba unali ndi kutsatira Mzimu Woyera utabwer pa iwo. Ngati Mzimu Woyera akhala mwa inu, azadzutsa thupi lanu la nyama tsopano komaso panthawi yachiukitso. Mbali imodzi yamphamvu ya Mzimu Woyera ndi mphamvu yochiritisa. Kukhala odzadzidwa ndi mphamvu ya Mzimu imene imadzutsa ndikupereka moyo ndikuteteza machiritso. Masalimo 119:25,50. Werengani Masalimo 11 pamene kudzutsa kwa Mzimu kwatchulidwa ka 11.

OPANI MULUNGU:

Baibulo limalonjeza moyo wagwiro kwa onse amene amawopa Mulungu. Malaki 4:2; Aroma 8:15.

PANGANI UBWEZI WENI WENI NDI MULUNGU:

Popeza machiritso ndi “ali makupe Ake,”ndekuti mukuyenera kukhala pansu kaya mukufuna kapena mukutumikira machiritso (Malachi 4:2). “Pakukhala: mwa Ambuye, monga ngati nthambi ya mpesa, ndi ubwezi weni weni. Zimakulumikizitsani inu ku mpesa komwe “kuyamwa” kwa moyo ndi machiritso kumachokera.

YENDANI MUKUMVERA KWA MAU:

Ngati mukuyenda mukumvera kwa Mau, simungakhale mu tchimo ndipo izi zizachotsa matenda ameneme amabwera chifukwa chatchimo la munthu. Masalimo 38 imalemba zamubongo, kuthupi, kuuzimu, ndi maganizo zomwe zinachokera kutchimo la Davide.

Mulungu amakuyakhani inu poyang'anira pakumvera kwanu (1 Yohane 3:24). Kukhala molungama kumathandiza kupewa matenda amene amabwera chifukwa cha tchimo la inu eni. Kukhala molingana ndi Mau a Mulungu amaperekaso chitetezo kumatenda ena, monga ngati opatsirana pogonana. Kuyenda mkuvera kwa Mau a Mulungu ndikuphatikizapo kupemphera, kuwerenga, ndi kugwiritsa ntchito Mau. Onani Masalimo 128, Deuteronome 28, ndi Eksodo 15:26 ngati zitsanzo zamalonjezano a moyo wanthazi wakuthupi kwa onse amene amayenda mkuvera Mau.

TSATIRANI MALAMULO ACHILENGEDWE OKHUDZANA ZAUMOYO:

Zanenedwa ndi ma dotolo kuti 60% ya matenda amabwera kukuchokera pakukhala moyo wasasamal. Baibulo linadzadza ndi zitsanzo zotsatira malamulo achilengedwe okhudzana nthanzi. Mulungu yemweyo, “Ndine Mulungu amene ndimachiza iwe” anaperekaso malamulo monga ngati mbali imodzi ya Chipangano Chakale. Paulo anauza amuna amene anali mngalawa kuti adye chifukwa cha umoyo wawo (Machitidwe 27:34). Anamuza Timoteo kuti azimwa vinyo mmalo mokumwa madzi oyipa (1 Timoteo 5:23).

Thupi ngakhaleso mzimu ndi zopatulika chifukwa ndi kachisi wa Mulungu. Kupuma kokwanira, kuchita masewero olimbitsa thupi, ndikudya moyenera zimakuthandizani kuti muziyenda muthanzi lakumwanba chifukwa mukugwirizana ndi malamulo achilengedwe a Mulungu. Chifukwa chakuti thupi lanu ndi Kachisi wa Mzimu Woyera, musamaikemo zinthu zina zonse zonyasa monga ngati mowa, fodya.

ZINDIKIRANI BWINO THUPI LA KRISTU:

Mwaphunzira kale kufunika kwa kuzindikira bwino thupi la Kristu mgonero. Baibulo lamati ambiri adwala ndi kufoka chifukwa sanachite izi.

PAMENE MUKUDWALA, KHULUPIRIRANI KUTI MULUNGU AKUFUNA KUKUCHIZANI:

Khulupirirani kuti Mulungu akufuna kukuchizani, ngakhale kuti simunalandire machiritso. Kupereka ndikuwoneretsera zosiyana. Kupereka kwa chipulumutso kunachitika zaka zambiri inu musanachirandire ndipo chinawonetsedwera mwa inu. Kukhulupirira ndi kulimba mtima mukuperekedwa ngakhale kuwonetsera (kwa machiritso) sanafike. Kukhulupirira ndikosiyanana ndikutenga.

“Kukhulupirira” kukhulupirira Mau a Mulungu, koma osamakana zachilengedwe, zizindikiro zowoneka. Musamke mkumalengeza zizindikiro zanu mwakufuna ndi kumakweza chiwembu cha satana thupi mwanu koma ngati mwafusidwa, nthawi zonse yakhulani mwachilungamo. “Ndiri ndizizindikiro zamavuto amtima” kapena “adotoro andiyeza andipeza ndi mavuto amtima.” Yakhani pofusa ku Mau a Mulungu— “Ndimikwigwiriam Yake ine ndachiritidwa.”

Izi zikutsatira chitsanzo cha Yesu, amene sanakane chowonadi. Yesu ananena moveka bwino, “Lazaro wamwalira...Koma ndipita kuti mkamudzutse.” Ndikhani yobvuta kuika pamodzi chowonadi ndi chikhulupiriro.

MVOMERANI MULUNGU, KUPYOLERA MWA YESU NGATI NCHIRITSI WANU:

Tchimo ndi matenda ndi ndi ana amapasa a satana. Chipulumutso ndi machiritso ndi zoperekedwa ndi Mulungu. Kalvare asanabwere, anthu amkapulumuka ndi kuchiritsidwa kupyolera poyang’ana ku ichi mwachikhulupiriro. Kodi munamulandira Yesu yekha kukhala Mpulumutsi, kapena munamulandira Iye ngati nchiritsiso? Kodi angakutetezeni bwanji inu ku tchimo ngati simunamulandire Iye ngati Mpulumutsi? Nde angakutetezeni inu bwanji kumatenda ngati simunamuvomereze Iye ngati ntchiritsi?

Yesu anatenga matenda anu ndipo anasenza madwale anu panthawi yomweyo ndepakuchita choncho ananyamulaso machimo anu (Mateyu 8:17). Sitikuyenera kuyiwarira zokoma Zake, zimene ndikuphatikazo machiritso (Masalimo 103:1-3). Mulungu anaika tchimo ndi nthenda pa Yesu pakutifera. Ndetinganene bwanji kuti mbali imodzi ndi yathu pamene inayo siyathu?

Pa Aroma 10:9, mau oti “kupulumuka” ndi chimodzi modzi mau amene anagwiritsidwa ntchito ndi Marko pamene anati “Monga ambiri anamukhudza Iye ana lungamitsidwa.” Chipulumutso ndi mamasuridwe kuchokera ku tchimo ndi chilango chake. Kudwala ndi mbali imodzi ya chilango. Liwu la chi Giriki “sozo” limanyamula tanthauzo la machiritso akuthupi ku uzimu.

Mukhoza kumasuridwa kumsinga wa tchimo nthenda. Amakhululuka zolakwa zanu ndi kuchiritsa thenda zanu zonse (Masalimo 103:3). Ichi nchifukwa chake Yesu anati, “Kodi chopweka nchani : Kukhululukira machimo kapena kuchiritsa?” (Marko 2:9).

KUZANI CHIKHULUPIRIRO CHANU CHAMACHIRITSO:

Kusowa kwachikhulupiriro kumatchinga machiritso, ndemukuyenera kuti mukulitse chikhulupiriro chamachiritso. Sichithu chofunika kungokhala munthu wachikhulupiriro, monga munthu wakachikhulupiro kochepe mwa Mulungu wamkulu. Chikhulupiriro ndikukhulupirira Mulungu kuti *akuchiritsani, osati angathe kukuchiritsani*. Satana amakhulupirira kuti Mulungu angachiritse, koma amafuna kukuletsani inu kuchowonadi choti amachiritsa,

Chikhulupiriro chanu ndinjira imodzi yamachiritso, koma chifukwa ndi njira imene Mulungu amagwiritsa ntchito, ndikubwino kumaimanga iyo:

-Chikhulupiriro chochiza si:

-Chikhulupiriro chimene mmapulumuka nacho.

-Chikhulupiriro chamakolo anthu.

-Chikhulupiriro cha mwanokha, zotsatira zakukhulupirika kwanu, mwachitsanzo, “Ine ndilkuchita mbali yanga, naweso uchite yako.

-Chikhulupiriro chochiza ndi:

-Chikhazikitso cha zinthu zoyebezereka, chiyesero cha zinthu zosapenyeka.

-Kuyembezero Mulungu kuchita zomwe analonjeza.

-Chikhulupiriro chikhoza kukhala:

- Chikhulupiriro cha munthu amene akupempherayo.
- Chikhulupiriro cha yemwe akufuna machiritso,
- Chikhulupiriro cha nzako.
- Chikhulupiriro cha abale.

Chikhulupiriro chamachiritso chimadza pakumva Mau a Mulungu okhudzana machiritso. Kukumbukira zomwe munakumana nazo zimalimbikitsa chikhulupiriro chanu, koma kumva Mau a Mulungu kokha kumakuza chikhulupiriro chanu. Yesaya anayamba ndi chaputala chachiwombolo ndi mau oti “Ndindani amene wakhulupirira uthenga wanthu?” kukhulupirira uthenga, akuyenera kuti amve kaye. Aroma 10:17 imati chikhulupiriro chimadza pakumva Mau a Mulungu. “Liwu mu vesi imeneyi ikutathanuza “kuyakhula kwapaderadera kwa Mulungu” kumene mukhani ya umoyo wabwino---ikanakhala ndime imene imakhudzana ndi machiritso.

GWIRITSANI NTCHITO ZIDA ZAKHONDO YAUZIMU:

Kumbukirani kuti matenda ndi chiwembu cha satana pa thupi, monga mmene liriri tchimo pa moyo. Nkhondo yolimbana ndizimenezi ndi zida za khondo ya uzimu (Aefeso 6:10-18). Zida zanu ndikuphatikizapo kusala kudya ndi kupemphera (Yesaya 58:6-8). Pazoonjera pophonzira za zida zauzimu, onani phunziro lasukulu ya Harvest International phunziro lotchdwa “*Ndondomeko za uzimu: Buku lakamenyedwe ka nkhondo ya Uzimu.*”

MVOMEREZANI NJIRA ZA MAKHWALA NDI ZAKUTHUPI:

Pamene moto wayamba, simangoyitana bungwe lowona zozimitsa moto, magwiritsa ntchito china chirichonse chopezeka kuzimitsira moto (ndowa za madzi, kuthira madzi padenga, ndizina zotero). Pamene mwadwala, simangoyitana Mulungu yekha komaso magwiritsa ntchito chinachirichonse chopezeka kuti mumenyane kulimbana ndi matenda: adotolo, makhwala, kupuma, kudya moyenera ndi kuchita masewero olimbitsa thupi. Zonse ndi zinthu zochokera kwa Mulungu. Yamikani mmen machiritso amabwerera, koma perekani matamando kwa Mulungu!

Pewani kuwonjeza kuwiriku:

1. Kupemphera mapemphero amachiritso okha:

Akhristu ena amangodalira pemphero lokha, amakana chithandizo china chirichonse chochokera kumakhwala opangidwa munjira yamakono omwe ndi ndikukuza ubwino wa Mulungu. Yesaya anagwiritsa ntchito mbulu wamkhuyu pamachiritso (Yesaya 38:10-21). Yesu anati “odwala amafuna nsing’anga” (Luka 5:31) ndipo Luka, analinso nsing’anga, anali gawo lautumiki wa Paulo (Akorose 4:14).

Akhristu ena atenga mau apa 2 Mbiri 16:12-13 monga ngati umboni oti asamapite kwa adotolo chifukwa Asa atapita kwa asing'anga anafa. Koma mau akulu mu ndime imeneyi ndi "lokhalo" tchimo la Asa linali lakuti sanafune Yehova. Mu nthawi yazowa zazikulu za munthu, anayang'ana kwa munthu basi. Chikhulupiriro chake chonse anaika mwa munthu, ichi nchomwe analakwitsa.

Dotolo wazamankhwala ndi kukuza kwa chifundo cha Mulungu. Dotolo akhoza kuzindikira, koma akuyenera kudikira mphamvu ya kumwamba kuti ichize. Dokotala amagwira ntchito mogwirizana, osati motsutsana ndi Mulungu. Ma dotolo amachotsa amachotsa zonse zimene zimatchinga machiritso ndipo amapereka makhwala aoti achize. Madotolo achikhristu, mwapaderadera, amagwira ntchito bwino mogwirizana ndi Mulungu.

Makhwala ambiri amapangidwa kuchokera kuzitsamba ndi zinthu zina zimene zinalengedwa ndi Mulungu pachiyambi peni peni. Kuyamba mwapempherera makhwala musanamwe kumakukwa mphamvu yake kuti agwire ntchito bwuno kwambiri. Nchifukwa chakuti kumasala zimene Mulungu muzifundo zake anapereka mudera la nthandizo la makhwala? Ndizosamveka ngati kuletsa kuyenda kwa magari mitsempha kenako mkumafuna kuepemphera basi kapena kukana kuchotsa chotupa pachala chanu nde mkuitana akulu ampingo kuti abwere azakupemphereni. Zikhoza kukhala zonsamveka kukana kugwiritsa ntchito zachilengedwe kapena makhwala omvomerezeka komaso kumakana kudya chakudya tsiku ndi tsiku kuti mukhale ndi moyo ndi nthazi.

Zindikirani: Pakhale kusamalitsa posakha dotolo, makamaka panthawi imene pali matenda odwalika kwambiri. Ndikofunika kupeza yemwe amadziwa chowonadi chakuti kumwamba kumalowerera ndipo asamuzungulire munthuyu ndi nyengo yokamba zokhumudwitsa.

2. Kupereka malire mmene Mulungu amachiritsira ku makhwala atsopano:

Madotolo ndi makhwala amabweretsa machiritso kwa matenda ndiposo amathaniza mavuto amaganizo ndi amaganizo, koma sangathane ndi mavuto auzimu ndi ena omwe amadza chifukwa cha ziwanda. Makhwala nthawi zina amabisa mvuto leni leni ndipo samathana nalo. Machiritso akumwamba amathana nazo zonsezi.

KUCHITA MAWU

1. Izi ndi zina mwazitsanzo zam'Baibulo mmene Mulungu anagwirira ntchito yomasulu anthu ku mphamvu yoyipa zomwe zingagwiritsidwe ntchito pamachiritso auzimu

Kulowerera kwakumwamba: Atumwi anamasuridwa ku ndende ndi mngelo. Izi zikhoza kufanana ndi machiritso akumwamba: Machitidwe 5:17-21; 12:1-11.

Kulowerera kwa mphamvu yachilengedwe zomwe zinaikidwa ndi Mulungu:

Chimvomerezi chinamumasula Paulo ndi Sila mndende. Ichi chikhoza kukhala chitsanzo chamachiritso ochitika kupyolera mozochitika zachirengedwe zomwe zinaikidwa ndi Mulungu: Machitidwe 16:25-40

Kulowerera kwa akatswiri: kutulutsidwa ku ndende kunachokera kwa akuluakulu. Kugwiritsa ntchito izi ku makhwala, zikhoza kukhala chisamaliro choperekedwa ndi akatswiri amakhwala: Mschitidwe 16:35-39

Nthawi yakumfa: Mbiri inalemba kuti Petro ndi Paulo onse anaikidwa mndende ku Roma nchaka cha 67 A.D. nthawi imeneyi kunalibe zakumwamba, zachilengwedwe, kapena akatswiri kuluwerera. Onsewa anamphedwa. Gwiritsani izi ntchito kumachiritso, izi zikhoza kufanana ndimatenda otengera ku imfa.

Zonse zochitikazi zimathaniza kumvetsa bwino chowonadi cheni cnehi. Monga momwe Mulungu amafunira nthawi zonse kuti amasuke anthu kuchoka ku ndende, Amafunaso kuchiritisa. Nthawi zina akhoza kukhala machiritso akumwamba, achilengedwe omwe aikidwa ndi Mulungu, kupyolera muthanzo laakatswiri, kapena---kupyolera mukumasuridwa kotheratu---imfa. Palibe mkangano pakati pa ndondomeko pamene chikhulupiriro chikufa ndi champhamvu monga ngati chikhulupiriro cha moyo.

Machiritso onse amphumphu amachokera kwa Mulungu, kaya kpyolera mupemphero, makhwala, kapena muzochitika zachilengedwe. Malemba amaphunzitsa pamene Mulungu akuchita zozizwa, Alinso chimodzimodzi wamachawi pazochitika zochiza zomwe tingafotokoze ndi kulosera. (Onani Masalimo 65 yomwe imafotokoza mphamvu ya Mulungu imene ikh=ugwira ntchito mundondomeko ya chilengedwe yapa dziko lapansi.) Chinthu chofunika mkuzindikira izi ndikumpatsa Mulungu ulemerero chifukwa chamachiritso.

...Iwo sanazindikire kuti Ine ndamene nawachiza iwo. (Hoseya 11:3)

2. Onaniso ndondomeko zakakhalidwe mu Ufumu zomwe zaperekedwa mu phunziroli. Onani zitsogozo zomwe zikuyenera kukwaniritsidwa mmoyo mwanu:

___Mvomerezani Yesu Khristu monga Mpulumutsi.

___Mpatseni Mulungu kachisi Wake.

___Yambani mwafuna Ufumu wa Mulungu.

POMALIZA

Mwafika pamapeto pa kuphunzira kwanu zokhudzana ndi nkondo ya yathupi, koma nkondoyo izamenyedwabe mpakana kufikira patsiku limene inu muzachoke kudziko la uchimori, matenda, ndi imfa kupita pamaso pa Mfumu Yesu.

Ngati munali pansu pa chiwembu chakuthupi pamene mayamba phunziro lino, tikukhulupirira kuti chiphunzitsochi chabweretsa kale machiritso kwa inu kapena mwakozekera kuti mulandire. Kumbukirani: Inu muchiritsidwa—panopa kapena machiritso anu achedwerapo kapena mulandira machiritso omaliza pamene mukalowa mkupezeka kwa Ambuye.

Tikupempheranso kuti mawu amenewa akukhudzeni kuti inu muzitumikira machiritso ndi mamasuridwe kudziko lino lozuzika. Kuyambirira muntha kumanyalanyaza kutumikira machiritso, koma kumbukirani: Utumiki wamachiritso ndi wa onse amene amawotcha maulalo akusakhulupirira ndi matha amene alikumbuyo kwawo.

Nkhani imakambidwa yatsogoleri wina otchuka dzina lake Julius Caesar amene, analingalira zogonjetsa Britain, anayenda panyanja ndi asilikali ake kuchokera ku France kupita ku England. Atafika ku England awotcha galawa iriyonse imene anagwiritsa ntchito kuwolokera mtsinje wa English. Potero sikunakakhalanso kuthawa. Kunali kumenya nkondo kuti apambane kapena kumfa. Ichi chikuyenera kukhalaso maganizidwe anu ku utumiki wa machiritso.

Mutengapo mbali imodzi ya mbali ziwiri zokhudzana zimene mwaphunzira mu phunziro lino:

-Mukhoza kukhala ngati tsogoleri wa Muchipangano Chatsopano Gamaliyeri amene anayima mbali yotsutsa popereka chenjezo, kupereka mwayi kwa atspogoleri achipembedzo “kuti adikire ndi kuwona” njira imeyo.

-Kapena mutha kukhala ngati mtumwi Petro, yemweanapanga ukaziwotche. Anachiritsa munthu opuwala, anaputa mkwiyo wa atsogoleri achipembedzo, ndipo anaima mkitsutsana ndi maulamuliro amene anamuza kuti asalalikireso kapena kuchiritsaso mudzina la Yesu.

Nthawi zonse kumbulkira: Inu ndi njira yamchiritso, osati ochiritsa. Ndinu mudutsiramo chabe mmene Mchiritsi amene ali mwainu amatuphuka kira kunja kwa..

... Anthu amene akuyandikira kumfa komaso sangapirire ululu.

...Anthu amene akhumudwa, alibe chiyembekezo, ndipo akozeka kuimika manja.

...Anthu amene ataya okondeka awo kapena avulazidwa ndi ena ndipo mitiama mwawo akulira ndi ululu.

... Anthu omangidwa ndi ma unyolo auchimo ndikuponderezedwa ndi ziwanda.

... Anthu amene akumana ndi imfa.

Simunaitanidwe kuti makatenge nthawi yanu kufotokoza zovuta ndi mafuso opanda mayankho amene akhoza kubwera muutumiki wamachiritso. Simunaitanidwe kuzayakha mafunso, koma

kuti mukatumikire machiritso. Monga ngati mmene machitira potumikira chipulumutso, siyani zotsatira za utumiki wa machiritso kwa Mulungu.

Tengerani malingaliro amtumiki F.F. Bosworth amene anati:

“Ine ndizalalikira Unthenga onse Wabwino ngati sindiwona munthu wina atapulumutsidwa kapena kuchiritsidwa ngati ndikhalabe ndi moyo. Ndakozeka kukhazikitsa chiphunzitso change pa Mau a Mulungu wosasitha, osati pazochitika.”

Kupyolera masamba a buku lino, taika mmanja mwanu kuthekera kochita chozizwa. Tadzala mbeu ya machiritso mmoyo mwanu. Ikufanana ndi mbeu mudziko lakuthupi. Kuti ikakwaniritse kubweretsa moyo, mbeyu ikuyenera kusamalidwa bwino.

Muphunziro lino mwapatsidwa mbeu yachozizwa yochokera ku Mau a Mulungu. Ndi mbeu yachikhulupiriro yokhudza machiritso. Monga momwe simungathe kufotokoza mmene mbeu imamerera ndi kukula kudziko lakuthupi, inu simungafototozde chinachirichonse pa phunziro lokhudzana ndi machiritso. Koma ngati mungaisamale mbeu imene yadzalidwa mmoyo mwanu ndi mzimu, izabweretsa moyo.

Pomaliza, nawo mafunso awiri amaliza:

Tikufunsa: “Kodi mbeu imeneyi mutani nayo?”

Yesu akufunsa: Kodi chopweka nchani kunena kuti, “Machimo ako akhu; lulukidwa” kapena kunena kuti “Dzuka uyende?”

ZAKUMAPETO A

KASATHULA MWAKAUNIUNI

Mndanda otsatirawu waikidwa kuti ukuthandizeni inu kuti mupanga kauniuni ndi kuti methane ndi zomwe zimayambitsa matenda. Mwapemphero lingalirani funso lirilonse. Pempheni Mulungu kuti akupatseni chidziwitso ndi bvumbulutso pamene muzakhala mukumaliza kauniuni ameneyu:

KUSATHULA UZIMU:

- Kodi munamulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanu?
- Kodi munamulandira Yesu ngati nchiritsi wanu?
- Mukhulupirira kuti Mulungu angathe ndipo azakuchiritsani?
- Kodi mawerenga Baibulo lanu tsiku ndi tsiku?
- Kodi mawerenga Mau a Mulungu okhudzana machiritso ndicholinga chokulitsa chikhulupiro chanu?
- Kodi mumafunsa lonjezano la machiritso lomwe liri Mau a Mulungu?
- Kodi zochita zanu ndi mau anu amawonetsera chikhulupiro kapena kukaika pamalonjezano a Mulungu?
- Kodi mukuika chidwi chanu pa zizindikiro kapena pamalonjezano a Mulungu?
- Kodi mapemphera tsiku ndi tsiku?
- Kodi mavomereza machimo anu kwa Mulungu ndikupempha chikhululukiro tsiku ndi tsiku?
- Kodi makhululukira ena ndikuwapempherera iwo?
- Kodi maziyesa nokha kawirikawiri pazomwe zimatchinga kuti pemphero lisayakhidwe, kuphatikazapo:
 - Tchimo la nthundu wina uliwonse.
 - Mafono mumtima.
 - Mzimu wosakhulukira.

- Kuzikonda
- Njala yofuna mphamvu, pemphero lokakamiza.
- Kuchitira khaza munthu amene ulinaye pa banja.
- Kuzilungamitsa nokha.
- Kusakhulupirira.
- Kusakhala mwa Khristu ndi Mau Ake.
- Kusowa chifundo.
- Chinyengo, kunyada, kubwereza kupanda phindu.
- Kusapempha mu dzina la Yesu.
- Zotchinga za satana.
- Kusayamba mwafuna Ufumu wa Mulungu.

- Kodi mukuphwanya mw adaladala chitsogozo cha Malemba?
- Kodi nthawi zonse malandira ndi kukozeke moyenera mgonero?
- Kodi mapembedza ndi okhulupirira ena nthawi zonse, mazizungirira nokha ndi zochitika zachikhulupiriro?
- Kodi panayamba pakhalapo kutenga nawo mbali pazamatsenga ndi agzigogo anu, makolo, kapena inu mwini? Ngati ndi choncho, munayambapo mwazikana ndi kupempherera nthemberero lina lililonse limene lilipo kuti lidulidwe?
- Munayambapo mwayikapo chidwi kwambiri pamachiritso athupi anu kusiyana ndi anzimu?
- Kodi mukungofuna machiritso akuthupi mmalo mofuna kuti thupi , moyo, ndi mzimu omwe?
- Kodi mukuika chidwi chambiri pa machiritso anu kusiyana ndi pa Mchiritso?
- Kodi munayamba mwathana nazo machitachita omwe amatchinga machiritso kuphatikizapo:

- Kusowa kwachiphunzitsa
- Kusakhulupirira
- Kusowa chikhulupiriro
- Kusowa mphamvu
- Tchimo la inu eni losalapidwa
- Kukana kuti mukozedwenso

- Kusowa kopanga chiganizo ndi chikhumbokhumbo
 - Mavuto okhudzana ndi kupempha
 - Kusowa chipiriro
 - Kusamvera mundondomeko yamachiritso
 - Kusazindikira thupi la Kristu
 - Kusatulitsidwa kwa mizimu yoyipa
 - Kukopera ntchito ya Mulungu
- Kodi munapereka thupi lanu (Kachisi wa Mulungu) kubwezera kwa Iye?
- Kodi Mzimu Woyera anadzadza nyumba yanu ya uzimu kuti potero ziwanda ziwanda sizingakhalemo?
- Kodi mayamba mwafuna kaye Ufumu wa Mulungu kuti machitso machiritso awonjezereke kwa inu?
- Kodi mukugwiritsa zida zanu za uzimu pakhondo yathupi? Izi mkumphatikizapo:
- Mau a Mulungu.
 - Mwazi wa Yesu.
 - Mau awumboni wanu.
 - Ulamuliro omanga ndi kumasura.
 - Kupemphera ndi kulambira.
 - Zipangizo za zakhondo ya uzimu.
 - Ulamuliro ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
 - Dzina la Yesu.
- Kodi munayitanapo akulu ampingo kuzakupemphererani kutsatira malamgizo a Yakobo 5:13-18?
-
-

KUSATHULA ZAKUTHUPI:

- Posatengera mmene chuma chiriri, kodi mmadya magulu onse azakudya?
- Kodi nthawi zonse mumadya kwambiri kapena pang'ono?
- Kodi muli ndi mvutto losadya chakudya chabwino?

- Kodi munayamba mwayezedwapo kunyetchera, kapena chinachirichonse chakuthupi chokhudzana ndi kudya moyenera?

Lembani mndandanda wamadyedwe anu abwino:

- Kodi magona mokwanira?
- kodi machita masewera olimbitsa thupi kawirikawiri?
- Kodi masuta fodya?
- Kodi mmamwa zithu zoledzeretsa?
- kodi matenga makhwala ozunguza bongo?
- kodi matenga nawo gawo mmachitachita achiwerewere (machimo ogonana monga ngati chiwerewere, kugonana amuna kapena akazi nokhankha, ndizina zotero)?
- Ngati muli pamakhwala, kodi mmamwa monga mmene munauzidwira?
- Kodi ndinu otseguka ku machiritso amakhwala ndi achilengedwe?

Lembani mndandanda wamomwe mungakozere mavuto amene alembedwawa:

KUSATHULA ZA MAGANIZO NDI ZAMUBONGO:

- Kodi munachotsa “chikhalidwe cha anthu” chimene chitha kukutchingani kuti musalandire machiritso? (Onani chaputala 7 ndi 12 cha buku lino). Izi mkuphatikizapo zikhulupiriro ndi mafunso opanda mayankho otsatirawa:
 - Machiritso ndi zozizwa sizamasiku ano.
 - Nchifukwa chani akumfa onse samadzutsidwa?

- Ngati machiritso akumwamba amagwiradi ntchito, nchifukwa chani Akristu amamwalira?
 - Makhwala amakono amachititsa kuti machiritso akumwamba akhale opanda pake.
 - Machiritso akumwamba amaphunzitsidwa ndi mipingo yonyenga.
 - Thupi ndi lomwe lapatsidwa chidwi kwambiri kuposa moyo.
 - Ndi chifuniro cha Mulungu kuti inu mudwale.
 - Ichi ndi chizuzo cha olungama.
 - Machiritso akumwamba ndi osowa.
 - Matenda ndi nthanda wanu.
 - Matenda ndi minga mthupi mwanu.
-
- Kodi pali anthu, malo, nthawi za nyengo mmoyo mwanu zomwe mazipewa kapena kuzikana?
 - Kodi munawakhululukira ena amene amakupwetekani?
 - Kodi munazikhululukira nokha pamachimo ndi zolephera?
 - Kodi muli ndi tsankho?
 - Kodi muli ndichina zotchinga zirizonse zimene zimalumikizana ndi zomwe zinachitika kale?
 - Kodi muli ndi mantha opanda pake?
 - Kodi muli paubwezi ndi machitidwe pazithu zowononga, machitachita kapena maubwezi?
 - Kodi muli ndi chikhalidwe chosokoneza?
 - kodi maziyang'anira nokha pansi?
 - Kodi makhala nthawi zonse osangalala?
 - Kodi muli ndi mzimu wamtendere?
 - Kodi mulindivuto lothana ndi kunenedwa?
 - Kodi makonda kutsutsa, kukwiya, kapena kupsya mtima changu?

- Kodi muli ndi nkhwawa komaso matha okhudzana ndi tsogolo lanu?
- Kodi kukhala kwanu moyo kukuwoneka kopanda tanthauzo komaso kosasangalatsa?
- Kodi munayamba mwazuzidwapo kuthupi, pogonedwa, mmaganizo, kapenena maganizo ndi wina wake? Kodi munathana ndi mmene mumavera kwa iwo?

Lembani mdandanda wokozerera mavuto omwe akambidwa mndandanda wapitawu:

ZAKUMAPETO B

MAZIKO A M’BAIBULO A MACHIRITSO NDI MAMASULIDWDE

Gwiritsani Zakumapeto kuti mupitirize maphunziro anu maziko a machiritso ndi mamasulidwe

MAINA A MULUNGU AMU CHIPANGANO CHAKALE

Yehova-Jireh	Ambuye apereka	Genesis 22:14 CC: Afilipi 4:19
Yehoha-Nissi	Ambuye mbendera yanga	Eskodo 17:8-15 CC: Yohane 15:13
Yehoha-Shalom	Ambuye Mtendere wathu	Oweruza 6:24 CC: Aefeso 2:14
Yehova-Raah	Ambuye m’busa wanga	Masalimo 23:1 CC: Yohane 10:11
Yehoha-Tsidkenu	Ambuye chilungamo chathu	Yeremiya 23:6 CC: 1 Akorinto 1:30
Yehova-Shammah	Ambuye ali pano	Ezekieli 48:35 CC: Ahebri 13:5
Yehova-Rapha	Ambuye mchiritisi	Eskodo 15:26 CC: Yakobo 5:15

PEMPHERO LA AMBUYE LAMACHIRITSO

Pamene mukupemphero pemphero lachitsanzo lomwe linaperekedwa ndi Yesu lotchedwa “Pemphero la Ambuye,” liri ndi pempho la machiritso:

“Atate wathu muli kumwamba”: Pamene mukupempha kwa “Atate wathu” mukupempha pa maziko pa matanthauzo a mayina Ake onse, kuphaikidzirapo “Ambuye mchiritisi wathu.”

“Ufumu wanu udze, monga kumwamba chomwecho patsi pano”: Kumwamba kulibe matenda kapena machimo. Tikuyenera kuchita chifuniro cha Mulungu pano padziko monga mmene kumwamba kuliri, chomwecho timenyana ndi mateda komanso machimo.

“Mutipase ife lero chakudya chathu cha lero”: Yesu anati “mkate” ndi wa ana (okhulupirira). Machiritso ali mbali ya chakudya cha ana Mateyu 15:21-28).

“Mutikhulukire ife zochimwa zathu monga ifenso tawakhulukukira amangawa athu”: Ndime iyi imakamba za machiritso auzimu.

“Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa oyipayo”: Matenda akuyeenera kukanizidwa monga momwe muchitira ndi mayesero.

MKOMBERO WACHIEONONGEKO

Mulungu anati adzachiritsa ndi kubwenzeretsa zomwe dzombe, chirimamine, ndi anoni anawononga (Yoweli 2:25). Chirimamine ndi anoni ali mgulu la dzombe.

Zitatu zonsezi ndi zazing’ono msimkhu, zochuluka mukawerengero, ndipo ziri mu gula lowononga kwambiri la tizilombo. Kachilombo kenakalikonse kamadusa mumasiteji ofanana a madzila, mphutsi, papa, ndi kukula. Tizilombo tikakula timayamba kuyikira madzira a m’badwo wamtsoyolo. Pali mkombero osatha wachiwonongeko.

Chifukwa cha tchimo, pali mkombero wosatha omwe ukugwira ntchito pa dziko lapansi. Ndikudzera kwa Mulungu yekha kumene zotsatira za dzombe, chirimamine ndi anoni a uzimu zitha kuchiritsidwa.

KUCHITA NDI THUPI, MOYO, NDI MZIMU

Matenda a...	Machiritso a m’Baibulo	Machiritso a Chirengedwe
Uzimu (Tchimo)	Kuvomereza ndi Kulapa. Chipulumutso kudzera mwa Yesu	Palibe
Thupi	Pemphero la chikhulupiriro pa machiritso akuthupi. Mamasulidwe zikakhala kuti zinayamba ndi ziwanda	Machiritso achirengedwe Machiritso a kuchipatala*
Maganizo	Pephero la mzchiritso a mkati Mamasulidwe zikakhala kuti zinayamba ndi ziwanda. Kuvomereza ndi kulapa pa mtima wolakwika. Kukhulupikira ena. Kubwezeretsedwa kwa anthu ena, ngati kuli koyenera.	Uphungu
Maganizo	Mutha kupemphera pempherola machiritso ngati achitika chifukwa tizilombo toyambisa matenda	Uphungu kapena mamasulidwe ngati akakhala anayamba ndi ziwanda

*Mankhwala a kuchipatala amagwira ntchito ngat mabvuto anayamba ndi tizilombo toyambitsa matenda. Mankhwala sagwira tchito ngati mabvuto anayamba ndi ziwanda.

Mwachidule:

Mchiritso onse ovomerezeka amachokera kwa Mulungu, kaya kudzera mu pemphero, mankhwala, kapena njira yachirengedwe. Malembo amatisimikidzirfa kuti pamene Mulungu

akupanga zozizwitsa, alinso ochitachita mu zinthu zomwe zimachitika pa dziko lapansi zomwe titha kufotokozaka kapena kulosera. Machitsanzo, onani Masalimo 65 omwe amakamba za mphamvu ya Ambuye yomwe ikuchitachita pa dziko lapansi. Chofunikira ndikudzindikira izi ndikumupasa Mulungu ulemerero pa machiritso osatengeraf njira yomwe machiritsowo afikira.

... koma sanadziwa kuti ndinawaciritsa. (Hoseya 11:3)

MTENGO WAMA CHIRITSO

Mu Cibvumulutso 22:2, Yohane akukamba za mtengo wamu chipangano chatsopano umene masamba ake ali ochiritsira mitundu ya anthu. Madziko ake ndi madzi amoyo omwe:

- Ndiwoyera
- Ngati mwala wonyezimira wa kulusitalo
- Ukuyenda kuchokera kumpando wachifumu
- Wa Mulungu ndi wa Mwanawankhonsa.

Malo a mtengo muzinda oyera, kumbali iyi yamtsinjewo ndi kumbali inayo, mkati mwa dzinda. Zikunenedwa kuti:

- Mtengo wa Moyo
- Yobala zipatso zokolola maulendo 12
- Sunali osabereka, umabala zipatso mwezi
- Uliwonse.
- Masamba a mitengoyo ochiritsira mitundu ya
- Ya anthu.

Ogonjetsa ali ovomeredzedwa kudya zimpatso za mtengowu (Chibvumbulutso 2:7; 2:14). Zotsatira za kudya ndi:

- Sikudzankhalanso themberero:
Cibvumbulutso 22:3
- Akapolo a Mulungu adzachita utumiki
Wopatulika kwa iye: Cibvumbulutso 22:3
- Sipadzakhalanso kubuula, imfa, kupweteka,
Kulira, kuwawidwa, malingaliro oyipa (Zakale
Zapita): Cibvumbulutso 21:4
- Zonse ndin'zatsopano: Cibvumbulutso 21:5

Matanthaunziro ena ambiri a baibulo akuwonentsa kuti mtengo umenewu umagwira ntchito ngati mankhwala (Weymouth); kuchiritsa(Moffat); ndipo umakhala ndi zinthu zochiritsira (Williams).

MAWU OPHUNZIRA

Mawu ophunzira otsatirawa achitika pamene pama chitinda kawundula ndi kukodzekera phunziro ili:

NTHADZI LABWINO:

Mawu awa agwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chotsapano chokha. Mawu achi giriki “hugiaino.” Akukamba zokhala ndi nthadzi labwino, kuveka mu nthadzi labwino ngati mu 3 Yohane 2. Mu Macitidwe a Atumwi 27:34 chipulumutso chikutanthaunziridwa mu “nthadzi labwino.”

KUCHIRITSA, MACHIRITSO:

Mu Chipangano Chakale, kuchiritsa koyamba kunachitika mu Genesis 20:17 pamene Mulungu anachiritsa Abimeleki. Kukugwiritsidwa ntchito kokwana ka 65 mu Chipangano Chatsopano. Kuchiritsa kukunenedwa ngati kubwedzeretsa kukhala bwinobwino.

Kumuuza Mulungu kufuna machiritso ndizinthu zoti zimachitika chitika:

- Ndichiritseni, chifukwa mafupa anga
Agwedezeke: Masalimo 6:2
- Ndichiritseni, ndipo ndidzachiradi: Yeremiya
17:14
- Simatenda a anthu okha amene
amachiritsidwa, komanso madzi oyipa: 2
Mafumu 2:22, Ezekiyeli 47:8; Yeremiya 19:11
- Kuchiritsa anthu amitundu kumafunikira kuti
Mulungu akhululuke pamene amitundu alapa
zoyipa zawo: Hoseya 6:1; Yeremiya 30:17
- Ngakhaletso midzinda yakunja itha kuziwa
zamachiritso awa pamene yalapa: Yeremiya
51:8-9
- Aneneri onyenga amasusika chifukwa amangothana ndi ziwonetsero zokha koma osati
zakuya zeni zeni zaumzimu zomwe zimapweteka anthu: Yeremiya 6:14; 8:11

Mu Chipangano Chatsopano, aneni a mawu amenewa ndi:

- Therapueno: kuchita ntchito kapena
Kuthandidza. Kusamalira odwala,
Kuthandiza, kuchidza, kuchiritsa.
Nthawi zambiri anagwiritsidwa ntchito
mu Mateyu ndi Luka, kamodzi mu
Yohane 5:10 ndiposo kutantha mu
bukhu la Macitidwe a Atumwi
anagwiritsiratso mu bukhu la
Cibvumbulutso 13:3 ndi 12 lokha.
- Iaomai: kuchiritsa, kupanga zonse za
uzimu ndi kuthupi kukhala kwangwiro.
- Chitsanzo za machiritso akuthupi:
Mateyu 15:28. Agwiritsidwa ntchito

ka 22 mutanthauzo limeneri.
-Zitsanzo zamachiritso awu mzimu:
Mateyu 13:15; Yohane
12:40; Macitidwe a Atumwi 28:27;
Ahebri 12:13; 1 Petro 2:24.
-Sozo: Kupulumutsa kuchokera
kumatenda ndizosatira zake. Onani
Marko 5:23 ndi Luka 8:36
mwachitsanzo chabe.

-Diasozo: Kupulumutsa komaliziratu.
Onani Luka 7:3

Mayina a mawu awa akuphatikidza:

-Therapeia: Amakhudza za kusamalira
ndi kuwonetsa chidwi (Luka 12:42).
Zosatira zamasama a mtengo wa
moyo: Civumbulutso 22:2

-Iama: Njira yochiritsira. Yagwiritsidwa
ntchito ngati mawu ochulukitsa mu 1
Akolinto 12:9,28,30.

-Iasis: Ndiwofanana ndi muneni #2.
Akukamba za dongosolo ngati kufikira
kutsirizidwa (Luka 13:32; Macitidwe a
Atumwi 4:22,30).

KUCHIDZA:

Mawu awa sanagwiritsidwe ntchito mu Chipangano Chakale. Mu Chipangano Chatsopano dzina loti “iasia” likutathaunza kuti kuchiritsa, kuchidza: Luka 13:32; Macitidwe a Atumwi 4:22; 4:30. Muneni “therapeuo” akutanthauza kutumikira mu Macitidwe a Atumwi 17:25; kuchiritsa, kubwezeretsa moyo wanthadzi, ndi kuchidza mu Mateyu 17:16,18; Luka 7:21; 9:1; Yohane 5:10; Macitidwe a Atumwi 28:9.

KUDWALA:

Mawu awa agwiritsidwa ntchito mu Chioangano chatsopano kokwana ka 60 mu bukhu la ahebri. Koyambirira amapezeka mu Genesis 48:1. Pali kufanana kumatanthauzo, kuphatikizapo chofowoketsa, kukhala bwino pang’ono, kuchita koposa muyezo ndikukhala ofowoka. Dzina loti “matenda” linachitika kokwana ka 23 mu Chipangano Chatsopano ndipo akufotokodzedwa ngati zowawa mu Yesaya 53:3-4. Ena amatanthauzira kuti masautso ndi matenda. Tanthauza la matenda laperekedwa mu Deuterenomo 7:15.

Mu Chipangano Chatsopano, kudwala kwagwiritsidwa ntchito ngati mneni ndi:

-Asthenes: kukhala olema, ofowoka,
Osathekera, kudzadza ndi matenda.

-Kammo: Kukhala olema ndizotsatira zakugwira
ntchito mowirikidza: Ahebri 12:3; Yakobo
5:15. Kulema mumalingaliro kumaphinya
kuchira kuthupi.

-Sunecho: kumangidwa kapena kukhala
musinga za matenda, kukhala kapolo.

Amagwiritsidwaso ntchito ngati perekedzi:

-Asthenes: kukhala opanda mphamvu,
ofowoka, olema.

-Arrhostos: ofowoka, odwalako, odwala.

Zinthu zamayina ndi:

-Asthenia: Chofooketsa, thenda.

-Nosos: Matenda.

MATENDA:

Mawu awa sanagwiritsidwe ntchito mu Chipangano Chakale, koma mu Chipangano Chatsopano
ndi:

-Asthenia: Kufuna kuphamvu, chofooka,
kusakhala ndikuthekera kopereka
zipatso: Aroma 8:26; 2 Akolinto 11:30;
12:5,9,10. Mu Luka 13:11 ndi “mzimu
wa Matenda” umene umapereka
matenda kuchokera kwa Satana mwini.

-Asthenema: Kufowoka kwa
chinkhulupiriro: Aroma 15:1.

NTHENDA:

Mu Chipangano Chakale nthenda ya mapazi inantchulidwa mu 1 Mafumu 15:23 ndi 2 Mbiri
16:12. Nthenda yamatumbo inanenedwa mu 2 Mbiri 21:15. Nthenda imaziwika ndi:

- Fano lonyansa: Masalimo 38:7
- Choipa : Masalimo 41:8
- Kukula : 2 Mbiri 16:12
- Pena osachiritsika: 2 Mbiri 21:18

Aneni otsatirawa anagwiritsidwa mu Chipangano Chatsopano:

- Asthenes: kusowekera mphamvu, kukhala Olema, kudwala.
- Echo Kakos: kukhala odwala or kugwidwa ndi matenda.

Panali mitundu ya matenda ambiri. ina yosaneneka: Mateyu 4:24; 14:35; Marko 1:32-34; Luka 4:40. Zina zotsaziwika: Mateyu 9:20. Yesu anachiritsa nthenda zonse: Mateyu 4:23; 9:35; 14:35; Marko 1:32; Luka 6:17; 9:1; Yohane 5:4; 6:2.

MASAUTSO:

Monga momwe agwiritsira mu chigiriki, izi sizikutathauza kuti kurephera kuthupi. Zikutathauza kuti mabvuto, zowawa, ukapolo ndi mikwingwirima.

YAKOBO 5:13-18

Anthu amovomera mabvuto munjira imodzi mwaziwiri ngati izi:

1.Ena amavomeredza mabvuto ngati masautso: ngati mwasaukitsidwa (kuyesedwa, zowawa, mayereso) mukuyenera kudzipheperera nokha. Munthaso kupepha ena kuti apephere nanu, koma sayitanidwa kuti apepherere kuti mabvuto ano achoke. Malemba akunena kuti mukuyenera kupephera pamene mwasaukitsidwa chifukwa mukuyenera kuphunzira pomwe mukupephera nokha mumayesedwe anu komanso mumayeresero kuti mukaziwe mene mungagonjetsere.

2.Ena amavomereza kuti mabvuto ndi chitsangalalo: chitsangalalo chawo sichifukwa chamabvuto okha, koma pakati pa mabvuto amakhala ndikuthekera kosangalala mwa Ambuye, pakudziwa kuti Iyeo akuchita chita munyengo zonse.

Akulu ampingo akuyenera kuyitanidwa kuti azapepherere odwala. Ziwani kuti ndizoposa wakulu wampingo modzi. Munjira imene ulemero wama chiritso umapita kwa Mulungu osati kwa munthu. Odwala akuyenera kuyitana akulu ampingo pamene akuwonetsera machitidwe a chikhulupiriro ndi mapephero akuyenera kuperekedwa. Ikuenera kukhala pephero la chikhulupiriro, yochita kwakuya, ndi kuperekedwa ndi munthu olungama. Eliya akugwiritsidwa ngati chitsanzo cha munthu olungama amene amaziwa kupephera pephero la chinkhulupiriro ndilochita koposa. Kudzambiri onani 1 Mafumu 17:1; ndi Luka 4:25. Odwala akuyenera kupulumutsidwa (kuchokera kumatenda awo akuthupi), kuzusidwa (kubwezeretsedwa mphamvu), ndi kukhulukidwa kwa machimo (machiritso aku Uzimu).

Ndime imeneyi ikuwonetsa kuti pali kulumikizana kweni kweni pakati pa ntchimo ndi matenda zimapezeka mugawo ena (onani Masalimo 41:4). Pali za Uzimu, ngakhaleso zaku thupi, milingo yama chiritso. Zimaonetseraso mene umodzi ndi Ambuye umagwirira ntchito. Timatumikira ndipo Iye amamasula.

MACHIRITSO OMWE YESU ANAMUCHIRITSA MUNTHU

Pamene Mphamvu Zaziwanda Zikunenedwa

	Mateyu	Marko	Luka
Mkadzi wopeteka		13:10-17	
Munthu mzimu oipa	1:23-25	4:31-37	
Ziwanda ku Gadara	8:28-32	5:1-13	8:26-33
mkadzi wavuto lamagaz	i 9:20-23	5:25-34	8:43-48
mwana wa ziwanda	15:21-28	7:24-30	
mwana ndizimu oipa	17:14-21	9:14-29	9:37-43
chowanda chosaykhula	9:32-33		
chiwanda chosaona ndi chosayakhula	12:22-30		
	27 11:14-26		

FUNDO ZOPHUNZIRA:

Zotsatirazi ndi fundo zomwe mungaphunzirepo pa machiritso amene panali mphamvu za ziwanda zomwe zikuwonetseredwa mwa anthu.

Mkadzi wopeteka: Luka 13:10-17

Mzima ameneyu anali omangidwa kapena wopeteka:

Kuthupi: Msana wake unali opendeka (Satana amapanga izi kwa ife kuti mawonedwa anthu akhale owona panso malo mowona mwamba.)

Ku Uzimu mawonedweso anthu amakhala owona panso malo mowona mwamba.

Maganiziridwe: anawuzidwa kuti palibe chiyembekedzo

Zachuma: anagwiritsa zonse zomwe anali nazo.

Mzimayi uyu amapezeka pamapephero pa tsiku la sabata ndi Yesu anamuyitana kuti “mwana wa Abulahamu” (Agalatiya 3:7). Titha kuganizira kuti anali olungama, owopa Mulungu, komabe mzimu wamatenda unamanga kwa zaka 18.

Gawo ili likuwonetsa kufunikira kwa mzimu wachiziwitso pamene mukutumikira machiritso. Awa anali matenda amene anaperekedwa ndi Satana. Mu utumiki wake, Yesu anasiyanitsa pakati pa matenda abwino bwino akuthupi, amene amachirisika pakuyala mwanja kapena kuzoza ndi mafuta, ndiposo pena pamasautso aziwanda.

Mu nyengo zina okhulupirira amamangidwa kuchokera mkati ngati zotsatira za masautso aziwanda, mizimu yomangidwa imamasulidwa. Ngati anali otsakhulupirira amene anali ndi masautso akuthupi amene zotsatira zake zinali kukhala ndi ziwanda, ziwanda zimatulutsidwa. Yesu amafunsa “kodi zimayi uyu ngosayenera kumasulidwa?” (Yesu akadali kutifunsa kuti “Kodi odwala siwoyenera kuchiritsidwa?”)

Mamasulidwe a mzimayi ameneyu anachitika panthawi imene mapephero amachitika mwamatsiku onse. Zinabweretsa zotsutsa zambiri kuchokera kwa otsogolera muuzimu, kuphatikizirapo otsogolera mkachisi. Pakuthana ndiziwanda pakadali pano kumapereka kuwilingula kuchokera kwa azitsogolera ampingo. Ena amakana kuti zimapezeka. Ena amakana mphamvu yophinya ndikutenga ulamuliro mu thupi lamunthu. Yesu anayika manja ake pa mzimayi omangidwayu. Mpopo popo, anakhala owongoka ndipo analemekedza Mulungu. Mu utumiki weni weni wa kuphinyika ndiziwanda, Mulungu akuyenera kulandira ulemerero, osati munthu amene akugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu kuti akamasule anthu.

Munthu wogwidwa mzimu woipa m’sunagoge: Marko 1:23-28; Luka 4:31-37

Ngakhale munthu ameneyu anapezeka m’sunagoge ku kaperna, Yesu sanamunene kuti mwana wa Abulahamu kapena kuwonetsa kuti anali osatira wa Mulungu. Pakhoza kupezeka anthu mupingo amene ali anthu otsakhulupirira ndiposo okhala ndi ziwanda. Kupezeka anthu ambiri mupingo sizikutanthauza kuti ndikubadwa mwatsopano kapena kukhala omasuka kumphamvu za ziwanda.

Yesu amaphunzitsa ndi ulamuliro pamene ziwanda zimalira mofuula, “Tiri ndi chiyani ife ndi inu, Yesu wa ku Nazarete? Kodi mwadza kudzationonga ife? Ndikuziwani, ndinu Woyerayo wa Mulungu.” Chiwanda chinatenga lemba lomwe liri mu Masalimo 16:10. Kukhala ndiziwanda uku kunali kwakuchuluka, komwe kukunenedwa kuti “ife” kuwonetsera kupezeka kwakuposa chiwanda chimodzi. Ziwanda zimagwira ntchito magulu. Chiwanda chimodzi chinali woyimirira azake, chomwe chianti “Ine.”

Pamene chiwanda chimayamba kuyankhula, Yesu amaziresa ponena kuti, “khala bata (khala chete), ndipo tuluka mwa iye.” Ziwanda zimamupweteka munthuyu, zimalira ndi mau ofuula, mutaye pansu, ndikutuluka mwa iye.

Anthu amene amachitira umboni zochitika zimene anali odabwitsika ndi ulamuliro ndi mphamvu imene Yesu amathanira ndi mzimu yoipa. Anali odzizwa ndipo anafunsa kuti “ndichani ichi?” zonena zonse ndi mbiri inafalikira posepose monga zotsatira zake.

Chiwanda chaku Gadara: Mateyu 8:28-32; Marko 5:1-13; Luka 8:26-33

Malingani ndi Mateyu, anthu awiri okhala nazo ziwanda zovuta kuti panalibe munthu amene amatha kuwakhazika bata, amakhala kumanda. Marko ndi Luka anakamba za nyengo yovuta ndi mamasulidwe a modzi mwa iwo, amene nyengo zake zinali zovuta kwambiri zomwe Yesu anakumana nazo mu utumiki wake.

Kukhala pamenepa kunali kwaziwanda zambiri. Amuna onse anakuzidwa kwambiri pakana samatha kukhala moyo wabwino mumadera awo. Amakhala kumanda. Ziwanda mwamunthu modzi zimazintcha “chigawo” pakuti zinali zambiri. Zinapangitsa kuti munthu ameneyo kukakhale kovuta kumukhazika bata, ngakhale kumumanga ndizingwe kunali kovuta.

Ziwanda zinamuzuzwa kwambiri pakana amayenda yenda akulira mofuula, amazichekacheka ndi minyala, ndiposo samavala kalikonse. Sizofunikira kuziwa dzina la chiwanda kuti mukakhale nawo ulamuliro pa ichi. Ulamuliro wanu uli mu dzina la Yesu.

Ziwani mitundu ya ukapolo yomwe ili munkhaniyi:

Kuthupi:	kudula zingwe, kuzichekacheka
Malingaliro:	kulira mofuula
Za zinda:	analekanikitsidwa ndi anthu
Chikhalidwe:	samavala zovala
Uzimu:	Mitundu ya ziwanda

Ziwanda zinamuzindikira Yesu ndipo zinafunsa ngati Iye abwera kuzazizudza nthawi yawo isanakwane. “Nthawi yawo” kutanthauza chiwerudzo chawo chomalidza munganjo ya moto. Zinapepha kuti zinatimizidwa kunja kwa dziko ndimomwe zimanenera kuti mene Satana anawagawira madera awo. Yesu anawavomerredza kuti zikalowe mwa nkumba pamene Yesu anazitulusa. Izi zinapangitsa kuti nkumba zife. Anthu okhala muzindawu anamuuzwa Yesu kuti achoke mudera lawo. Nkhumba zinali ziweto zawo ndipo zinali zofunikira kwambiri kwa iwo kuposera kutulusa mphamvu zaziwanda mwa anthu.

Mkadzi wavuto lamagazi: Mateyu 9:20-23; Marko 5:25-34; Luka 8:43-48

Mkzadziyu anakhala munyengoyi kwa zaka 12. Anavutika zinthu zambiri zakuthupi ndipo anagwiritsa ntchito zonse zomwe anali nazo, koma zinakulirabe tsiku ndi tsiku malo moti zikhale bwino. Anali okakamira, chifukwa anazikakamidza muchigulu kuti akakhunze Yesu.

Anaziyankhulira yekha mwachinkhulupiriro ndiku ganizira atakhalanso bwino, osati machiritso okha. Anati “Ndizakhala bwino.” Chinali chinkhulupiriro chake, sikukhuza kwake, komwe kunamuchiritsa. Yesu anati, “Chinkhulupiriro chako chakupulumutsa. Pita mutendere. Khala omasuka kuthenda yako.”

Pamene zimayiyu anakhuza Yesu, mphamvu inachoka mwa Iye ndipo wonse anava. Anachiritsidwa nthawi yomweyo ndipo mpopo mpopo anava muthupi lake kuti wachiritsidwa kunthenda yake. Anachiratso kumalingaliro pamene anamasulidwa kuzowawa zake. Ngakhale Yesu nthawi zambiri amagwiritsa mzimu wachiziwitso, koma panthawiyi Yesu anagwiritsa ntchito njira zakuthupi. Anafunsa “Ndani wandikhudza?”

Mwana wa kadzi wachisurofoinike: Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30

Mwana wakadzi ameneyu inali ndi mzimu woyipa umene mayi ake amuwuzindikira pakuwonetsera kuthupi. Mzimayiyu anafotokoza kuti mwana wake kuti “wogwidwa ndi mzimu wongansa.” Yesu anachiritsa tsungwanayu chifukwa cha chikhulupiriro chomwe anawonetsa mayi ake. Tsungwanayu sanakhelepo pamene amapezeka Yesu, zomwe zikuwonetsera kuti kupeza kuthupi sikofunikira kuti munthu akamasulidwe pakuphinyidwa kapena kukhala ndi ziwanda za Satana.

Izi ndi zotsatirazi ndizinthu zomwe zimuwonetsa kuti ana amatha kukhuzidwa ndi Satana. Khani ngati iyi ikufotokodzato za ubwino waku chilimika ndiposo fundo zamachiritso kuti ndi “mkate wa ana” (izi ndiza ana a Mulungu).

Mwana ogwidwa ndi mzimu woyipa: Mateyu 17:14-21; Marko 9:14-29; Luka 9:37-45

Ophunzira anayesera kuturutsa mzimu woyipawu, koma analephera. Yesu anati izi zili chochi chifukwa chakusakhulupirira ndiposo kuti chiwanda ngati ichi chima choka ndikupephera komanso kusala kudya. Malo a anthu osakhulupirira kunapangitsa nyengoyi, pakuti ophunzirawa anazunguliridwa ndi osakhulupirira komanso kunali kutsutsana ndi atsogoleri azipembedzo panthawiyi.

Nkhaniyi ikuwonetseraso kuti pali mphamvu zaziwanda zosiyana siyana, zina zamphamvu kwambiri kuposa zizake. Maphatikizo amomwe nyamatayu angafotokozeredwe kuchokera mu baibulo zawonetseredwa motere:

- Anali ndiziwanda (otsokonedzeka malingaliro)
- Anali wa khunyu
- Amagwira pa moto ndi madzi nthawi zambiri (mzimu owononga)
- Mzimu umamupweteka kapena kumuvulaza
- Anali ndi mzimu osayakhula
- Mzimu umamungamba
- Amakukuta mano
- Panali kusaukitsika mwakuthupi
- Anayamba izi ali mwana

Munthu ayenera kukhala wosamalitsa posagonjetsedwa ndi osamva komanso osalakhula kapena amene ali ndi ziwanda. Pali ambiri amene ali osamva komanso osalakhula amene alibe ziwanda. Mwina kutheka anadwalapo kapena kuvulala zomwe zinagwitsa mavutowo.

Luka akunena kuti pamene nyamatayu anabwera kwa Yesu, chiwanda chinamupangitsa kuti akhale ndi mphamvu, koma Yesu anazuzula mzimuwu ndi kuchiritsa mwanyu. Mateyu anati Yesu anazuzula satana, ndipo chinachoka, ndipo mwanayo anachira nthawi yomweyo.

Marko akunena kuti kukumana ndichiwanda kumeneku ndikodabwitsa kwambiri kuposa kwa Mateyu ndi Luka. Yesu anafunsa mafunso atate wake kuti kwa nthawi yayitali bwanji nyamatayu wakhala ndi ziwanda. Atate wake anati zinayamba ali mwana wang'ono.

Yesu ananena kwa atate wake kufunikira kwaku khulupirira, kenako anayakhula ndi mzimu wosamva komanso osayankhula ndipo anachiuza kuti chituluke ndikuti chisankhaleposo. Mzimu unalira ndipo unatuluka kumusiya munthu uja pamene anthu ambiri amaganiza kuti wafa, koma Yesu anatenga mkono wake ndikumuzusa.

Pamene ophunzira anamufunsa Yesu kuti ndichifukwa chiyani sananthe kutulusa chiwandacho, Yesu anayankha:

...Cifukwa cikhulupiriro chanu ncacing'ono; pakuti indetu ndinena ndi inu, Mukakhala naco cikhulupiriro monga kambeu ka mpiru, mudzati ndi phiri ili, Senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadakulakani kosacitika.

Koma, zinthu izi sizichoka chabe koma ndi pephero ndi kusala kudya. (Mateyu 17:20-21)

Yankho lake likuwonetsera kufunika kwa chinkhulupiriro, pephero ndi kusala kudya pakuthana ndi mphamvu yaziwanda. Zikusimikidzatso kuti ziwanda zina ndizovuta kuzitulutsa kuposa zina chifukwa Yesu anati “ZINTHU NGATI IZI sizichoka” popanda pephero ndi kusala kudya.

Fundo yosangalasa: Anthu anamukana Yesu (Yohane 1:11) pamene ziwanda zinamuziwa Iye (Luka 10:15).

Chiwanda chotsayakhula: Mateyu 9:32-33

Munthu uyu anabweretsedwa kwa Yesu ndi kusayakhula komwe kunachitika chifukwa anali ndi ziwanda. Pamene chiwanda chinatulutsidwa, munthu anakhala ndikuthekera koyankhula. Nkhamu linali lodabwitsikandipo linati, “Sizinawonekepo mu Israyeli.” Afalisi anamuwukira Yesu pochosa ziwanda kuzera mu mfumu ya ziwanda.

Chiwanda chosaona ndi chosayakhula: Mateyu 12:22-30; Marko 3:22-27; Luka 11:14-26

Kukhala apa zikuphatizaso masautso akuthupi omwe ndi kusaona ndi kusayakhula. Yesu anachiritsa munthu ameneyu pakutulutsa chiwanda mwa iye. Anali kutha kuyakhula ndi kuona pakutha pomasulidwa. Kunali kulumikizana kumeneku ndi mamasulidwe komwe Yesu anapereka ziphunzitso Zake zakuya zokhuza kutulutsa ziwanda. Tsatane tsatane wa chiphunzitso zikuwonetsa:

-Nyumba chogawanikana siyingakhalitse.
Ziwanda zimantcha matupi omwe zimakhala
kuti “nyumba.” Ndizosatheka kuti ziwanda
zikakhale nyumba imodzi ndi mzimu wa
Mulungu.

-Satana sangatulutse satana mzake.

-kutulutsa ziwanda ndi gawo limodzi la utumiki wa Ufumu wa Mulungu.

-Ziwanda zimatulutsidwa ndi Mzimu wa Mulungu.

-Tichoyenera kumanga munthu wamphamvu (Satana) pamene mukufuna kuchitulutsa (mosokeneze ntchito yake).

-Pali malo ofanana ochitira nkondo mu uzimu. Ngati sumili ndi Yesu, ndiye kuti muli mbali yotsutsana naye.

-Pamene zimu oyipa watulutsidwa Mwamunthu, umafunafuna kuti ukalowetso muthupi lamunthu.

-Ngati munthu amene wachosedwa chiwanda sangazaze nyumba yake ya uzimu ndi Mzimu Oyera, chiwanda chikabwerera ndi ziwanda Zina. Malo mwake muthusi akasitha kuposa kale.

Zichito chito zina:

Pakuwonjedzera maumboni omwe aperekdwewa, baibulo limapereka ndemanga zokhuzana ndi utumiki wa Yesu kwa onse omwe anakhunzidwa ndi mphamvu ya ziwanda.

-Maumboni otsatirawa mawu oti
“kuchiritsidwa” agwiritsidwa ntchito
pakukamba zamene Yesu anathanira ndi
ziwanda: Mateyu 4:24; Luka 6:18

-Maumboni otsatirawa mawu oti “kutulutsa”
agwiritsidwa ntchito pakukama za njira Zake:
Marko 1:32-34,39; 6:13

-Luka 4:41 kunena kopweka kuti ziwanda
“Zimatuluka.” Luka 7:21 akunena kuti Iye
“Anawachidza” onse. Mateyu 8:16 akunena
kuti Iye “anazitulutsa ndi mawu Ake.”

-Marko 16:9 ndi Luka 8:2-3 amati Yesu
anatulutsa ziwanda 7 mwa Mary Magadareni.

-Munkhamu la anthu, Yesu sanalole kuti
ziwanda zikayankhule: Marko 1:32-34

MACHIRITSO AMENE YESU ANAMUCHITIRA MUNTHU

Pamene Mphamvu Ya Ziwanda Siyinakambidwe

	Mateyu	Marko	Luka	Yohane
Apongozi				
Ake a Petro	8:14-15	1:30-31	4:38-39	
Wakhate	8:2-4	1:40-42		5:12-13
Wamanjenje	9:1-8:35	2:1-5	5:17-26	
Wopuwala				
Dzanja	12:9-35	3:1-5	6:6-11	
Mwana wamkadzi				
Wa Yairo	9:18-19	5:22-24		8:41-42
	23-26	35-43		49-56
Munthu osamva				
Ndi osalakhula	7:32-37			
Munthu osaona	8:22-26			
Batumeyu wakhungu	20:30-34	10:46-52	18:35-43	
Kapolo wa				
Konturiyo	8:5-13		7:1-10	
Ankhungu				
Awiri	9:27-30			
Mwana wamkadzi				
Wamasiye	7:11-15			
	Mateyu	Marko	Luka	Yohane
Munthu				
Wasanje	14:1-6			
Akhate 10	17:11-19			
Khutu lakapolo	22:49-51			
Mwana wa mkuru			4:46-53	
Zosantheka			5:1-47	
Obadwa ndi nkhungu			9:1-14	
Lazaro			11:1-44	
Mkadzi ogwidwa				
Ndichigololo			8:1-11	
Mkadzi ochimwa	7:36-50			

MAWU OPHUNZIRA:

Zotsatirazi ndi mawu omwe mwaphunzira pamachiritso a munthu omwe alibe mphamvu ya ziwanda:

Apongozi ake Petro: Mateyu 8:14-15; Marko 1:30-31; Luka 4:38-39

Anamuuza Yesu zakufuna chosowaku. Iye anabwera, nawagwira zanja, nawazutsa, ndipo malungo anawachokera. Pena zimanena kuti Iye anamukhudza zimayiyu, nayimba pambali naye, nazuzula malungo. Anadzuka ndipo anawatumikira iwo.

Wakhate: Mateyu 8:2-4; Mark 1:40-42; Luka 5:12-13

Wakhateyu atamuwona Yesu, anabwera akulambira koma akufunsaso. Anati “Ngati inu mufuna.” Yesu anati, “Ndichita.” Uyu ndi munthu modzi yekha amene anafunsa cholinga cha Yesu ngakhale amafuna machiritso. Yesu nthawi yomweyo anamusimikizira iye, “kuti ndichita.” Yesu anasunthika ndikukhuzidwa ndipo anatambasula zanja lake ndi kukhuza iye. Yesu anamuuza kuti asawuze munthu aliyese koma apite kukaziwonetsa yekha kwa wa nsembe ngati umboni. Ananyamuka, ndi nthawi yomweyo anakhala wabwino bwino.

Wamanjenje: Mateyu 9:1-8; Marko 2:1-12; Luka 5:17-26

Mphamvu ya Ambuye inali pamalopo ku chiritsa chifukwa choti Yesu anayakhula za Mawu a Mulungu kwa iwo. Afarisi, aphunzitsi a malamulo ndi Alembi analiso pamalopo, koma machiritso anabwera kudzera mu Mawu, osati kwa ophunzitsa ndi atsogoleri a mpingo.

Munthu odwalayu analowesedwa kudzera pa denga ndi azizake. Azizake amenewa anali “abale mukumasulidwa.” Kodi Mulungu akufuna akugwiritseni ntchito kuti “Mukachose denga” kwa munthu amene ali osowa?

Panali zophinja zambiri zomwe zimayenerera kugonjetsedwa:

-Nkhamu la anthu: lomwe limantchinga njira yopita kwa Yesu. Kodi ndichontchinga chiti chamunthu pakati pa inu ndi mamasulidwe anu?

- Mayendeseredwe a kumano: Machitidwe awo amasokoneza mayendetseredwe a kumano. Tisamangike kusata dongosolo kapena ndondomeko yomwe siyikafikira zotsowa za anthu.

-Zinthu zofunikira: denga limayenera kuperekedwa ngati nsembe. Udindo wanthu, maganiziridwe anthu, katundu wanthu zikuyenera kuyikidwa kaye pambali kupereka njira ya mamasulidwe.

-Mawonedwe azinthu: Anabweretsa mzawo kuma Chiritso. Yesu anati “Munthu iwe, macimo ako Akhululukidwa.” Amayenera kusiya kumbali Mawonedwe awo azinthu azomwe amafuna kuti Zichitike kapena momwe amafunira kuti zikhalire Kuti chipulumutso chikachitike.

Yesu anawona chikhulupiriro cha azizakewo, koma odwala anali chophinja kuti chikhulupiriro chake chomwe. Munthu ameneyu amadwala kuthupi komasno anali odwala ku uzimu komwe kunaza chifukwa cha uchimo. Koyamba Yesu anathana ndi nthenda kaye. Pamene kukambirana kumapitirira pakati pa anthu kuti Yesu anali nawo ulamuliro ochita izi kapena ai. Yesu anati, “Ndinena kwa iwe...” tikuyenera kuva mawu a Yesu pamwamba pa nkhamu la anthu otsakhulupirira omwe atizungulira kuti tikalandire mamasulidwe anthu.

Chinkhulupiriro cha azizakewo chinayambitsa dongosolo lama chiritso. Anzanu antha kukubweretsani kwa Yesu, koma nthawi zina mukamakhala muli nokha. Munthu amayenera kusiya zofooka zonse zakale kuyambatso mwatsopano kuzera mukuvera. Akuyenera kutenga Kama lake nayenda.

Pamene Yesu anamuuza kuti ayime, atenge Kama lake, ndikupita kunyumba kwake, kwa nthawi yomweyo ananyamuka napita akulemekedza Mulungu. Kudwabwitsidwa ndi mantha anali mayankho a mboni kumachiritso.

Munthu wa dzanja lopuwala: Mateyu 12:9-13; Marko 3:1-5; Luka 6:6-11

Machiritso awa anachitika patsiku la sabata pamene Yesu amaphunzitsa mu m’sunagogi. Inali nthawi yamayesero, pamene

ZAKUMAPETO C

FOMU YAKAUNIUNI

Pakuti yesu ndi dokotala wankulu, ndi chitsanzo cha utumiki wa machiritso ndi mamasulidwe. Gwiritsani ntoto fomu iyi ndi zitsanzo zomwe mwapatsidwa mu Zakumapeto B kuti mupitirizebe kuphunzira utumiki wa Yesu:

1. **Fotokozani munthu yemwe akufuna machiritso ndi mamasulidwe:**
 - Ngati dzina lake linaperekedwa, ndi liti?
 - Kodi zaka zake zinali zingati?
 - Mwamuna kapena mkazi?
 - Kodi anali ochita chani?
 - Kodi anali ochokera dziko liti?
2. **Fotokozani chomwe akufuna:**
 - Kodi chinaonetseredwa bwanji ndi anthu ena?
 - Kodi chinaonetseredwa bwanji ndi munthu yemwe akufuna machiritso?
3. **Kodi munthuyo amamufunsa Yesu kuti achite chani?**
4. **Kodi Yesu amasonyeza gwero la bvuto lamunthuyo?**
____Eya ____Ayi. Ngati eya, chinali chani?
5. **Kodi ndi ndani amatengapo kathu pa machiritso?**
 - Kodi munthu akufuna kanthu? Ngati eya, anachita chani?
 - Anthu ena? Ngati eya, anachita chani?
 - Yesu? Ngati eya, Anachita chani?
6. **Nthawi ya mutumiki:**
 - Kodi Yesu anati chani?
 - Kodi Yesu anachita chani?
 - Kodi Yesu anamuudza odwala kuti achite chani?
 - Kodi Yesu anati ndi malingaliro otani ofunika pa machiritso?
 - Kodi munthu yemwe amafuna machiritso anaonetsera chikhulupiriro?
 - Kodi anthu ena anaonetsera chikhulupiriro? Ngati eya, anaonetsera bwanji?
7. **Chitsimikizo cha machiritso:**
 - Kodi zidzindikiro cha kuthupi zinali zotani?
 - Kodi munthu amatani akachiritsidwa?
 - Kodi anthu ena amatani ku machiritso?
8. **Kulondola kwa machiritso:**
 - Kodi yesu amamuuza munthu kuti achitepo kanthu? Ngati eya, ndichani?
 - Kodi munthuyo amapannga chani?

Ndemanga ndi zolemba zina:

MAYANKHO A MAFUNSO OZIYESA NOKHA

CHAPUTALA 1

1. Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoonu pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe. (Eksodo 15:26)
2. Zigawo zikulu zikulu za zinthu zonse ndi zinthu zomwe ziri za kuthupi kapena zinthu zomwe ziri za kuuzimu. Onani 1 Akorinto 15:44-49
3. Ufumu wa Mulungu ndi Ufumu wa Satana.
4. Satana, ziwanda, dziko, ndi thupi.
5. Mulungu Atate, Yesu Khristu, Mzimu Woyera, ndi angelo.
6. Mawu oti “mfumu’ amatanthauza kuti olamulira dera kapena anthu.4
7. Ufumu ndi dera ndi anthu amene mfumu ndi olamulira.
8. Nkhondo ya uzimu ndi kusanthula kwa ndi kutengapo mbali pa nkhondo ya uzimu yosaoneka. Imakamba za kumphunzira za mphamvu zotsutsana zabwino ndi zoipa, njira za satana, ndi njira za uzimu zogonjetsera woyipao.
9. Chifukwa chimwene kuli nkhondo ndi chakuti Satana amafunitsitsa kukhala olamula wankulu. Akumenya nkhondo yolimbana ndi thupi, moyo, ndi mzimu wa munthu. Njira zake zikulunjika pa Mulungu, mapulani anke ndi Anthu ake.
10. Tikuyenera kudzindikira kuti nkhondo zonse za m’ moyo mwathu, kaya zakuthupi, maganizo, maganizo, chuma, zikungoonetsera za gwero la uzimu. ingakhale mu dziko la kuthupi zitha kumaoneka ngati zikuchitika kudzera muzochitika za m’ moyo, maziko a nkhondo zonse za kuthupi ndi dziko la uzimu.

CHAPUTALA 2

1. Ndipo muzitumikira Yehova Mulungu wanu, potero adzadalitsa cakudya cako, ndi madzi ako; ndipo ndidzacotsa nthenda pakati pa iwe. (Eksodo 23:25)
2. Kuchiritsa kwamaganizo: Mawu awa amagwiritsidwa pofotokoza machiritso a maganizo pa chinthu, ufiti, zinthumwa, ndi zamizimu zomwe sizili za m’Baibulo.

Machiritso auzimu: Pali magwero ena a machiritso auzimu omwe sachokera kwa Mulugu, ndiye sitigwiritsa mawu awa mu phunziro lathu. Satana atha kupanga machiritso auzimu (Eskodo 7:8-13).

Machiritso akuchipatala: Mtundu uwu wa machiritso umagwiritsidwa ndi madotolo, anamwino, kuzipatala, ndi makhwala. Pomwe tikhala tikuphunzira, njira yovomerezeka simatsutsana ndi Mawu a Mulungu kapena machiritso aumulungu, koma ndikutambasuka kwa ubwino wake.

Machiritso achilengedwe: Machiritso omwe amachitika kudzera mumatupi a anthu popanga chithandizo chirichonse chakuchipatala. Izi zimaonetsera khalidwe la Mulungu ndi ntcito yake mumatup a anthu. “Machiritso achirengedwe” amakambatso zakugwiritsa ntchito njira zachirengedwe monga chakudya chabwino, mavitamini ndi mchere wachirengedwe, kupuma kokwanira, ndi zina zotero.

Machiritso a chikhulupiriro: Mawu awa amagwiritsidwa ntchito pokamba za machiritso a Mulungu. Sitirigwiritsa ntchito, komabe, chifukwa limalnjika ku chikhulupiriro cha iye akutumikira kapena akulandira utumiki.

3. Mawu oti “umulungu” limalunjika kwa Mulungu, osati chikhulupiriro cha munthu. Komanso imatsiyantsidwa ndi zamatsenga ndi machiritso auzimu. “Umulungu” umakamba za Mulungu woona ndi chikhalidwechake, chomwe chimaonetsedwa mu Mawu Ake, Baibulo.
4. Machiritso amatumikiridwa ku matenda aku thupi ndi maganizidwe pomwe mamasulidwe amathana ndi matenda oyambitsidwa ndi ziwanda.
5. Yesu satume aliyense kukalalikira Uthenga Wabwino opanda osawalamulira kuti akatumikira machiritso ndi mamasulidwe. Kunalikuonetsera kwa mphamvu komwe kunapangitsa kuti Uthenga Wabwino wa Ufumu ufalikire ponseponse

CHAPUTALA 3

1. Mwananga, tamvera mau anga; Cherera makutu ku zonena zanga. Asacoke ku maso ako; Uwasunge m'kati mwa mtima wako. Pakuti ali moyo kwa omwe awapeza, Nalamitsa thupi lao lonse. Cinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; Pakuti magwero a moyo aturukamo. (Miyambo 4:20-23)
2. Awunyalanyaza, kuwukana, kuwuchedwetsa, ndi kuwubvutitsa ndi zikhulupiriro za anthu.
3. Onani zokambirana za mu Chaputala 3.
4. Onani Zokambirana za mu Chaputala 3.

CHAPUTALA 4

1. Kristu anatiombola ku temberero la cilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense woo paeikidwa pamtengo. (Agalatiya 3:13).
2. Imfa ndi matenda zinalowa mu dziko chifukwa cha kuchimwa kwa anthu oyamba, Adamu ndi Hava.
3. Satana.
4. Onani zokambirana za Chapulata 4.
5. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 4.
6. Mutha kumasulidwa ku temberero la matenda ndi imfa pakulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi.

CHAPUTALA 5

1. Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu. Kundikomera kuti ndinazunzidwa; Kuti ndiphunzire malemba anu. Sindidzaiwala malangizo anu nthawi zonse; Popeza munandipatsa nao moyo. (Masalmo 119:67,71,93).
2. Zifukwa zitatu za matenda zomwe zakamphudwa mu ohunzirori ndi:
 - Kuphwanya malamulo auzimu:
 - Kuphwanya malamulo a chilengedwe cha mulungu
 - Ziwembu za satana
 - kusazindikira kwenikweni thupi la khristu
 - Kuonongedwa kwa thupi kuti mzimu ukapulumuke.
3. Onani zokambirana za Chaputala 5
4. Onani zokambirana za Chaputala 5
5. Onani zokambirana za Chaputala 5
6. Onani zokambirana za Chaputala 5
7. Onani Zokambirana za Chaputala 5

CHAPUTALA 6

1. Mundicitire cifundo, Yehova; pakuti ndalefuka ine: Mundicize, Yehova; pakuti anthunthumira mafupa anga. Moyo wanganso wanthunthumira kwakukuru; Ndipo Inu,

Yehova, kufikira liti? Wamva Yehova kupemba kwanga; Yehova adzalandira pemphero langa. (Masalmo 6:2-3,9)

2. Matenda a uzimu, kuthupi, maganizo, misala, ndi aziwanda.
3. Matenda a uzimu ndi uchimo. Ngati simuthana nalo, mdula moyo wa uzimu.
4. Kudwala kukhoza kubwera chifukwa chakusokonekera kwa thupi. Ndi mavuto oti akhoza kuzindikiridwa ndikuwonedwa ndi akatswiri achipatala.

Kudwala kwa thupi kutha kubweranso chifukwa chakusokonera kapena kusagwira bwino kwa ziwalo zathupi. Awa ndi matenda amene amabwera chifukwa chakusokonekera kwa chiwalo chimodzi zomwe zimapangitsa kuti thupi lonse lisokonekere. Matenda odziwika bwino ndi monga matenda a mtima, kuthamanga kwa magazi, shuga, tizilonda tammimba ndi ena otero. Ngati matenda akhalitsa osachizidwa amatha kuwononga ziwalo zina. Chifukwa chakugwirizana kwa thupi la munthu, kudwala kwa mbali imodzi kukhoza kunkhudza thupi lonse.

5. Kudwala kwa maganizo kumabwera chifukwa chamaganizo oipa monga ngati mkwiyo, kuwawidwa mtima, ndi zina zotero. Kuti izi zichiritsidwe Mulungu akuyenera kukhudza maganizo amkati. Ena amawatchula kuti “machiritso amkati,” ngakhale mauwa nthawi zina amagwiritsidwa ntchito molakwika ndipo amakuzidwa mkumatanthauza zomwe Baibulo silimaphunzitsa.
6. Matenda amasila amayamba chifukwa chakudwalitsa nthawi yayitali, kukhumudwa, zilema zobadwa nazo ndi zina zomwe sizimabwera ndi satana.
7. Mwamatenda ena amene amabwera chifukwa cha ziwanda ndi monga kugwidwa ndi mizimu yoyipa, kuponderezedwa, komaso ziwanda zina zimachititsa munthu kudwala matenda amasila ndi matenda ena akuthupi.

CHAPUTALA 7

1. Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu, ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu adzukulu ndi ciyembekezero. (Yeremiya 29:11)
2. Matenda otengera ulemerero kwa Mulungu ndi matenda aku imfa.
3. Kumwalira nthawi isanakwane ndi kumwalira mu nthawi yake.

CHAPUTALA 8

1. Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu, natundudwidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife taciritsidwa. (Yesaya 53:5)
2. Onani zokambirana za Chaputala 8.
3. Onani zokambirana za Chaputala 8.
4. Ndime zotsatirazi zikutsimikiza kuti machiritso ndi mphoto ya nsembe ya Yesu Kkrstu.
 - Yesaya 53:45
 - 1 Petro 2:24
 - Masalimo 103:2-3
 - Mateyu 8:17
5. Onani zokambirana za Chaputala 8.
6. Ndime zotsatirazi zikutsimikiza kuti okhulupirira onse akuyenera kutengapo mbali pa machiritso ndi mamasulidwe.
 - Mateyu 10:1-42; 16:17-19; 28:16-20
 - Marko 6:7-13; 16:14-20
 - Luka 9:1-6; 10:1-24; 24:44-53
7. –Ngati kukhumba mtima chanu ndi Ufumu wa Mullungu, zone zofunikira zizapatsidwa kwa inu.
 - Kuti mulandire, mukuyenera kupereka.
 - Palibe chosatheka ndi Mulungu.

CHAPUTALA 9

1. Ndipo Iye anaturutsa mizimuyo ndi mau, naciritsa akudwala onse; kotero kuti cikwaniridwe conenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti, Iye yekha anatenga zofoka zathu, Nanyamula nthenda zathu. (Mateyu 8:16-17)
2. -Kuonetsera chikhalidwe cha Mulungu.
 - Kulemekeza Mulungu.
 - Kutsimikiza kuti Yesu ndi Mpulumusi ndi Wodzodzedwa.
 - Kutsimikidza nthenga ndi uthenga.
 - Kulimbikitsa malandiridwe a Uthenga Wabwino.
 - Kukhadzikitsa Ufumu wa Mulungu.
 - Kuonetsera chiweruzo pa mdani.
 - Kukuda azitsogoleri auzimu.
 - Chimwemwe chachikulu

CHAPUTALA 10

1. Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao. Pakuti kwa mmodzi kwapatsidwa... ndi kwa wina mphatso za maciritso, mwa Mzimu mmodziyo. (1 Akorinto 12:7-9)
2. Mzimu Woyera ndi mbali ya utatu wa Mulungu.
3. Onani chimaliziro cha Chaputala 10.
4. Mphatso zauzimu ndi kuthekera kwa uzimu koperekedwa ndi Mzimu Woyera kwa okhulupirira kuti akautimikire ngati mbali ya Thupi la Khristu.
5. Okhulupirira wa mphatso yamachiritso ali ndi kuthekera kutulutsa mphamvu ya Mulungu yobwezeretsa nthanzi pamwamba pogwiritsa njira za kuthupi. Anthu onse okhulupirira anatumidwa kukapempherera odwala, koma okhulupirira yemwe ali ndi mphatso yamachiritso amagwiritsidwa mwapaderadera ndi mowirikidza ndi Mulungu mu iyi ya utumiki.
6. -Kuphunzitsa ndi Kulimbikitsa
-Chinenero, Malilime amitundu mitundu, Mamasulidwe a malilime
-Chidzindikiro cha Mizimu
-Mphatso ya Chikhulupiriro
-Mawu a Chidziwitso
-Mawu a Nzeru
-Mphatso ya Machitidwe a Mphamvu
7. -Azibusa (Adzitsogoleri a uzimu): Ezakieli 34
-Akulu a mpingo/azitumiki: Yakobo 5:14
-Okhulupirira wana aliyense: Luka 16:15-18; Yakobo5:16
-Omwe ali ndi mphatso yamachiritso:1 Akorinto 12:9
-Mpingo wonse-ukuyenera kukhala malo amachiritso: Luka 14:16-24

CHAPUTALA 11

1. Moyo wanga umamatika ndi pfumbi; Mundipatse moyo monga mwa mau anu. Ndinafotokozera njira zanga, ndipo munandiyankha: Mundiphunzitse malemba anu. Mundizindikiritse njira ya malangizo anu; Kuti ndilingalire zodabwiza zanu. Moyo wanga wasungunuka ndi cisoni: Mundilimbitse monga mwa mau anu. (Masalmo 119:25-28)
2. Onanitso zokambirana za mu chaputala ichi pa miyambo zikhalidwe za anthu.

CHAPUTALA 12

1. Ndipo Yehova adzakantha Aigupto kukantha ndi kuciritsa; ndipo iwo adzabwerera kwa Yehova, ndipo Iye adzapembedzedwa ndi iwo, nadzawaciritsa. (Yesaya 19:22)
2. Baibilo limati anali wa Satana.
3. Munga m'thupi la Paulo inali nthenga wa Satana kuti kuti amutundudze.
4. Inaloledzedwa pa zifukwa zitatu:
 - Ikalepheretse tchimo.
 - ikakwaniritse uteneri.
 - Ikapereke mphamvu.
5. Ikamutundudze.i
6. Onani mndandanda wa maonetseredwe osiyana siyana omwe akambidwa mu Chaputala 12.
7. Paulo anayakhulapo za mazunzo ake kutanthauza kuti “amkasowa mphamvu, kufooka, kulephera kubweretsa zotsatira kupyolera mukuyesa yesa kwake.” Minga ya Paulo inawonetsera mphamvu ya Mulungu mmoyo mwake.

CHAPUTALA 13

1. Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici. (Deuteronomo 29:29)
2. Machitachita mu utumiki wa machiritso ndi zifukwa zomwe anthu ena amachiritsidwira pamen ena ayi.
3. Onani zokambirana za Chaputala 13

CHAPUTALA 14

1. Ndipo pamene mulikumuka lalikirani Ufumu wa kumwamba wayandikira. Chiritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwa ulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:7-8)
2. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 14.
3. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za CHaputala 14.

CHAPUTALA 15

1. Ndipo mwa ici ali Nkhoswe ya cipangano catsopano, kotero kuti, popeza kudacitika imfa yakuombola zolakwa za pa cipangano coyamba, oitanidwawo akalandire lonjezano la zolowa zosatha.

Pakuti pamene pali copangiratu pafunika pafike imfa ya wolemberayo. (Ahebri 9:15-16)

2. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 15.
3. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 15.

CHAPUTALA 16:

1. Cifukwa cace sitifoka; koma ungakhale umunthu wathu wakunja ubvunda, wa m'kati mwathu ukonzedwa kwatsopano tsiku ndi tsiku.

Pakuti cisautso cathu copepuka ca kanthawi citicitira ife kulemera koposa kwakukuru ndi kosatha kwa ulemerero;

Popeza sitipenyenera zinthu zooneka, koma zinthu zosaoneka; pakuti zinthu zooneka ziri za nthawi, koma zinthu zosaoneka ziri zosatha. (2 Akorinto 4:16-18).

2. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 16.

CHAPUTALA 17:

1. Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)
2. Mizimu ya zifooko, mizimu yokopa ponyengerera, ndi mizimu yonyansa.
3. Mphatso yozindikira mizimu ndiyofunika kwambiri polimbana ndi mphamvu ya ziwanda. Imakupangitsani kuti mukazindikire mwachangu ngati munthu ali ndi mizimu yoyipa kapene ayi. Imaletsa kunyengedwa pokopedwa kapena kumizimu yonama. Munthu yemwe ali ndi mphatso imeneyi antha kuzindikira machitachita oipa ndi malingalilo a mohamvu ya ziwanda.
4. Kuponderezedwa ndi ziwanda zikuthanthauza kuti mphamvu ya ziwanda imakuponderedza, kutsutsana nawe, kapena kukumanga kuchokera kunja.
5. Fananizani mndandanda wanu ndi mndandanda womwe waperekedwa mu Chaputala 17.

6. Kukhla ndi ziwanda zikutanthauza kuti wazadzidwa ndi zilakolako za ziwanda, Satana, ndi zamatsenga.
7. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 17
8. Kudzadzidwa ndi ziwanda ndi kakhalidwe kamene mzimu kapena mizimu yonyasa (ziwanda) imakhala mu thupi la munthu ndikutenga ulamuliro wonse.
9. Fananizani mndandanda wanu ndi mndandanda womwe waperekedwa mu Chaputala 17.
10. Fananizani yankho lanu ndi mndandanda wa mu Chaputala 17.

CHAPUTALA 18:

1. Ndipo pamene Iye anadziitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, anapatsa iwo mphamvu pa mizimu yoipa, yakuiturutsa, ndi yakuciza nthenda iri yonse ndi zofoka zonse. (Mateyu 10:1)
2. Onse obadwa mwatsopano.
3. Onani zokambirana za Chaputala 18.
4. Onani zokambirana za Chaputala 18.
5. Onani zokambirana za Chaputala 18.

CHAPUTALA 19:

1. Ciritsani akudwala, ukitsani akufa, konzani akhate, turutsani ziwanda: munalandira kwaulere, patsani kwaulere. (Mateyu 10:8)
2. Onani zokambirana za Chaputala 19.
3. Onani zokambirana za Chaputala 19.

CHAPUTALA 20:

1. Udzikondweretsenso mwa Yehova; Ndipo iye adzakupatsa zokhumba mtima wako. Pereka njira yako kwa Yehova; Khulupiriranso Iye, adzacicita. (Masalmo 37:4-5)
2. Fananizani yankho lanu ndi zokambirana za Chaputala 20.